

# ***CHOTUPITSA-NGATI***

## ***UVANGELI***

### **HARVESTIME INTERNATIONAL INSTITUTE**

Phunziro limeneri ndi gawo limodzi la maphunziro a **Harvest International Institute** ndipo cholinga chake ndi kukonzekeretsa okhulupilira kuti akatute zokolora zambiri zauzimu.

Mutu waukulu mumaphunzirowa ndikuphunzitsa zimene Yesu anaphunzitsa, zimene zinasandulitsa anthu wamba monga asodzi, otolera misonkho ndi ena kulalikira Uthenga Wabwino ndi kuwonetsera mphamvu ya uthengawo mu nthawi yawo.

Bukuli ndi phunziro limodzi mwa maphunziro ambiri amene cholinga chake ndikuwakopa okhulupilira kuti akakonze dongosolo, kuyendetsa, ndi kubweretsa pamodzi anthu kuti Uthenga Wabwino ukalalikidwe.

© Harvestime International

Institute <http://www.harvestime.org>



## ZAMKATI MWA BUKULI

Kagwiritsidwe Nthcito Ka Bukuli . . . . .	5
Ndondomeko Zothandizira Kuphunzira Limodzi Pagulu . . . . .	6
Chiyambi . . . . .	7
Zolinga Za Phunziroli . . . . .	9

### GAWO LOYAMBA: PITANI

<b>Chiyambi Cha Gawo Loyamba . . . . .</b>	<b>10</b>
1. Chotupitsa-Ngati Uvangeli . . . . .	11
2. Lamulo . . . . .	21
3. Uthenga . . . . .	30
4. Otumikira . . . . .	38
5. Kupereka Uthenga Wabwino . . . . .	46
6. Olandira Uthenga . . . . .	51
7. Njira: Mfundo Za Chipangano Chatsopano . . . . .	59
8. Njira: Mafanizo A M'chipangano Chatsopano . . . . .	68
9. Njira: Uvangeli Wa Panokha . . . . .	75
10. Njira: Kuthana Ndi Zovuta . . . . .	85
11. Njira: Uvangeli Wochulukitsa . . . . .	92
12. Njira: Mtsonkhano Wa Uvangeli . . . . .	101
13. Zisakho Kapena Ophunzira . . . . .	118
14. Kukonzekera uvangeli . . . . .	129
15. Kulumikizana pa uvangeli . . . . .	135

### GAWO LACHIWIRI: PAMENE MUKUPITA

<b>Chiyambi Cha Gawo Lachiwiri . . . . .</b>	<b>145</b>
16. Chiyambi Chamachilitso Ndi Mamasulidwe . . . . .	146
17. Zochitika Zomwe Zimasokoneza Machiritso . . . . .	170
18. “Pamene Mukumuka, Kachizeni” . . . . .	187
19. “Pamene Mukumuka, Kamasuleni” . . . . .	202

### GAWO LACHITATU: PAMENE MULI KUMENEKO

<b>Chiyambi Cha Gawo Lachitatu . . . . .</b>	<b>231</b>
20. Kubzala Mpingo: Chitsanzo . . . . .	232
21. Kubzala Mpingo: Njira Zoyenera . . . . .	238
22. Kubzala Mpingo: Kuchulukitsa . . . . .	253

Kumapeto: Mawu Omaliza . . . . .	261
Mayankho Amafunso Oziyesa Nokha . . . . .	264

# KAGWIRITSIDWE NTHCITO KA BUKULI

## KAKONZEDWE KA BUKULI

Phunziro liri lonse limakhala ndi zinthu izi:

**Zolinga:** Izi ndi zimene mukuyenera kukwaniritsa kapena kudziwa pa mapeto pa phunziro. Welengani zimenezi musanayambe phunziro lanu.

**Vesi Yotsogololera:** Ndimeyi imatsindika mfundo yayikulu mu phunziro lathu.

**Zopezeka mu Magawo:** Gwiritsani ntchito Baibulo lanu kuti mufufuze mavesi amene sanalembedwe mu bukuli koma angotchulidwa.

**Mayeso Odziyesa Nokha:** Osathamangira kulemamba mayeso musanamalize kuwerenga chaputala, komanso polemba musagwiritse ntchito Baibulo kapena bukuli polemba mayesowa. Mayankho amayesowa muwapeza kumapeto a bukuli.

**Zophunzira Zowonjezera:** Ndime imeneyi ikuthandizani kuti muwerenge mau Mulungu ndi kuzamitsa ukadaulo wanu pophunziro komanso kugwiritsa ntchito mu utumiki zimene mwa.

**Mayeso Omaliza:** ngati mwayamba kuphunzira phunziroli mukuyenera kulemba mayeso pamapeto a phunziroli ndipo mayesowo aperekedwa kwa aphunzitsi anu kuti mupatsidwe malikisi.

## ZOWELENGA ZINA ZOFUNIKA POHUNZIRA PHUNZIROLI

Mudzafunikira Baibulo

## NDONDOMEKO ZOTHANDIZIRA KUPHUNZIRA LIMODZI PAGULU

### MKUMANO WOYAMBA

**Kutsekulira:** Yamabani ndi pemphero ndi kudziwana wina ndi mnzake ndipo ophunzira alembetse mayina.

**Khazikitsani Ndongomeko Zapagulu:** Musankhe amene atsogolere mkumano wanu, sankhaninso malo ndi masiku amene mudzikumana.

**Mayamiko ndi Matamando:** Yitanirani kupezeka kwa Mzimu Woyera pamene muchita mkumano wanu.

**Gawani Mabuku Kwa Ophunzira:** Awuzeni ophunzira dzina laphunziro, zolinga zake ndi dongosolo.

**Perekani Nchito Yoyamba.** Ophunzira ayenera kuwerenga ma chaputala amene apatsidwa ndikulemba mayeso odziyesa okha isanafike nthawi ya mkumano wina. Ndipo kuchuluka kwa machaputala amene adziphunzitsidwa pa mkumano uli onse kuzitengera kutalika kwa chaputala komanso kumvetsetsa kwa ophunzira.

### MKUMANO WACHIWIRI NDI KUKUMANA KWINA PATSOGOLO

**Kutsekulira:** Tsekulirani ndi pemphero kenako lembani mayina awophunzira atsopano ndikuwapatsa buku lawo. Muyitane mayina a wophunzira amene abwera. Komanso osayiwala mayamiko ndi matamando kwa Mulungu.

**Kukumbutsira:** Yambani ndi kubwereza mwachidule zimene munaphunzitsa mu mkumano wanu womaliza.

**Phunziro:** Afunseni ophunzira ndemanga zawo kapena mafunso okhudza phunziro limene aphunzira komanso mmene angagwiritsire ntchito zimene aphunzira pamoyo wawo ndi utumiki.

**Mayeso Odziyesa Nokha:** Konzetsani mayeso amene ophunzira amaliza ndipo mukhonza kusankha kupereka mayankha kapena kuwachotsa mubukuli kuti ophunzira adzipezere okha mayankho.

**Mayeso omaliza:** Pamapeto pa maphunziro amenewa, gulu la ophunzira onse lidzapemphedwa kulemba mayeso omaliza ndipo aphunzitsi awonetsetse kuti ophunzira wina aliyense ali ndi buku laphunziroli.

**GAWO:** Uvangeli

**PHUNZIRO:** Chotupitsa-ngati Uvangeli

## CHIYAMBI

- Pafupfupi theka la anthu onse a dziko lapansi sananve Uthenga Wabwino.
- Anthu ochuluka sanafikiridwe ndi Uthenga wa Ambuye Yesu Nkhristu.
- Mitundu yambiri ya anthu sinalandire mamishonale.
- Pali zilankhulo za anthu zokwana pafupifupi chikwi chimodzi ndi mazana asanu ndi ziwiri zomwe zilibe Mau olembedwa a Mulungu.
- Chiwerengeru cha anthu a dziko lapansi chichuluka kwambiri pa dzaka zosapitirira makumi asanu zikudzazi.

Tikamaganizira chiwerengero ngati ichi pofuna kukwaniritsa utumiki waukulu ya Yesu Khristu, wotengera Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu kwa cholengedwa chinachirichonse, timadzindikira kuti tiri ndi ntchito yochuluka. Phunziro iri lalembedwa ndicholinga chofuna kuikidza pamodzi ndi kuphunzitsa anthu okhulupirira kuti akakwanirise ntchito yimeneyi. Ndi ntchito yayikulu, koma ndiyothekeka.

Maphunziro ambiri a uvangeli amalunjika pa lamulo “lopita” ku dziko ndi uthemga wabwino. Amatsindika kwambiri pa za kulalikira ndi kuphunzisa uthenga wabwino. Phunziroli ndilotsiyana chifukwa likulunjikanso pa zimene Yesu ananena zoti zichitike “pamene mukupita” ndi machitidwe azinthu a mpingo wa Chipangano Chatsopano “pamene muli konko.” Phunziroli lagawidwa mu zigawo zitatu.

**Gawo 1** ndi lotchedwa “Pitani.” Gawoli likulinjika pa lamulo lomwe Yesu anapereka lolalikira za uthenga wabwino wa Ufumu wa Mulungu kwa zolengedwa zones. Likuphatizanso malangizo a uthenga womwe ukuyenera kugawidwa, otumikira, m’mene Uthenga Wabwino ungaperekedwere, ndi olandira uthenga. Njira za uvangeli zaphunzitsidwanso, potsindikiza njira zomwe zinagwiritsidwa ntchito mu Chipangano Chatsopano. Uvangeli wa panokha ndi wochita ndi anthu ena wakambidwanso, ndi malangizo achindunji a m’mene tingathanire ndizovuta ndi m’mene tingawasatsamalire otembunika atsopano. Malangizo a makonzekeredwe ndi kasonkhansitse ka chuma cha uzimu komanso kalumikizandwe ndi anthu ena pa za uvangeli.

**Gawo 2** ndi lotchedwa “Pomwe mukupita.” Mu mabuku a Uthenga Wabwino mu Chipangano Chatsopano, Yesu sanangolamulira kuti anthu akalalikire Uthenga Wabwino okha komanso anawalamulira kuti akatumikire machiritso ndi mamasulidwe. Anawaudza kuti “Pomwe mukupita...chiritsani akudwala, tulutsani ziwanda...” (Mateyu 10:1,7-8). Pomwe khamu la anthu linabwera kuti lidzachiritsidwe ndi kuzamasulidwa, zokolora za uzimu zinayamba kuchuluka mofulumira kuti antchito ena anayamba kufunidwa. Sipanapite nthawi pomwe ophunzira ena makumi asanu ndi awiri anafunidwa ndipo anatomizidwa kukalaikira, kukaphunzitsa, kukachiritsa ndi kukamasula. Kunali kuwonesera kwa mphanvu uku “pomwe anapita” zomwe zinapangisa kuti uthenga wabwino ufalike mofulumira ku dziko lonse lapansi. Pachifukwa ichi, Gawo Lachiwiri la phunziroli lilunjika pa utumiki wa machiritso ndi mamasulidwe omwe angatsatane ndi kulalikira komanso kuphunzitsa za Uthenga Wabwino.

**Gawo 3** likulunjika pa matsatidwe a kachitidwe ka zinthu omwe awululidwa mu Chipangano Chatsopano “pamene muli kumeneko.” Likuonetsera kuti uvangeli si wathunthu pokhapokha mpingo wadzalidwa pakati pa otembunika atsopano. Uvangeli opanda kukhadzikitsidwa kwa mipingo ya m’madera ili ngati kubweretsa ana mu dziko koma kukana udindo wa chitsamaliro chawo. Munthu asatengedwe kuti walandira “uvangeli” pokhapokha atakhala

otenga nawo gawo mu nkumano wa mpingo wa m'madera. Kuti izi zikakwaniritsidwe, pakuyenera kukhala mpingo wa kudera. Dera sirikuyenera kuonedwa kuti linalandira uvangeli pokhapokha mpingo utakhazikitsidwa ku derako.

Magawo onse atatu aphunziroli akutchuridwa kuti “chotupitsa-ngati uvangeli” chifukwa uthega wabwino ukafalitsidwa mofulumira pa dziko lonse lapansi monga ngati chotupita chilowerera mtanda wa mkate. Chotupitsa chitha kukhala chochepa komanso chobisika, koma kukhudza kwake kulibe malire.



## ZOLINGA ZA PHUNZIROLI

Pomaliza pa phunzirori mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kutanthauzira chotupitsa-ngati uvangeli
- Kufotokoza lamulo la uvangeli
- Kulemba mwachidule utheka wa uvangeli  
Kudzindikira mtumiki wa uvangeli
- Kudzindikira wolandira utheka
- Kulankhula uthenga wabwino kwa anthu ena
- Kulemba mwachidule mfundo za Chipangano Chatsopano za uvangeli
- Kulemba mwachidule mafanizo a Chipangano Chatsopano a uvangeli
- Kuchita uvangeli pa inu wekha
- Kuthana ndi amvuto omwe mungakumane nawo pa uvangeli
- Kufikira dera lonse ndi uvangeli ochulutsa
- Kuchita mtsonkhano wa uvangeli
- Kuwayendera omwe atembenuka ntima kumene
- Kulemba zolinga za uvangeli
- Kulumikizana ndi anthu ena pa za uvangeli
- Kulemba mwachidule zimene Baibulo limaphunzisa pa za machiritso ndi  
mamasulidwe
- Kufotokodza zosintha zomwe zimakhudza machiritso
- “Pomwe mukupita, chiritsani”
- “Pomwe mukupita, masulani”
- Kufotokoza m'mene kabzalidwe ka mpingo mu Chipangano Chatsopano kamakhalira
- Kutsatira njira za Chipangano Chatsopano zobzalira mipingo
- Kutsatira njira za Chipangano Chatsopano za kachulukitsidwe ka mipingo

## CHIYAMBI CHA GAWO LOYAMBA

### “PITANI”

Gawo loyamba likulunjika pa lamulo la “pitani” ku dziko lonse la pasi ndipo mukalalikire Uthenga Wabwino kwa zolengedwa zonse zamoyo.

Mu gawo lino muphunzira za lamulo lomwe laperekedwa ndi Yesu kuti mukalalikire Uthenga Wabwino wa Ufumu ndi kulandira malangizo wa uthenga omwe ukukagawidwa, amithenga a Uthenga Wabwino, m'mene mungalankhulire Uthenga Wabwino, ndi olandira uthnga.

Muphunzira njira za uvangeli, potsindikiza njira zomwe zinagwiritsidwa ntchito mu Chipangano Chatsopano. Uvangeli wa panokha ndi wochita ndi anthu ena wakambidwanso, ndi malangizo achindunji a m'mene tingathanire ndizovuta ndi m'mene tingawasatsamalire omwe angotembunika ntima kumene.

Malangizo aperekedwatso a kadzalidwe ndi m'mene mungalankhulane ndi anthu ena ndi cholinga chopanga uvangeli.

Ndipo tsopano...kodi mwakonzeka “Kupita”?

## CHAPUTALA 1

### CHOTUPITSA-NGATI UVANGELI

#### ZOLINGA:

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba mavesi otsogolera
- Kutanthauzira “chotupitsa-ngati uvangeli”
- Kufotokodza “tanthauzo la otayika”
- Kufotokodza “tsogolo a anthu otayika”
- Kuzindikira masitepe asanu ndi imodzi a ndondomeko ya uvangeli

#### MAVESI OTSOGOLERA

**Ndiponso anati, Ndidzafanizira Ufumu wa Mulungu ndi chiani?**

**Ufanana ndi chotupitsa mikate, chimene mkazi anatenga, nachibisa mu miyeso itatu ya ufa, kufikira unatupa wonsewo. (Luka 13:20-21)**

#### CHIYAMBI

Phunzirori likufotokoza kufunikira kwa uvangeli, ndondomeko za uvangeli, ndi kutanthauzira mau omwe ndiofunika kuti inu mukanvese matchutchuchu pamene mukuyamba kuphunzira phunziroli. Pamene Kachisi ankamangidwa mu Chipangano Chakale, phokoso la nyundo, nkhwanga, kapena chipangizo chilichonse cha chitsulo silinanveke pamene limamangidwa (1 Mafumu 6:7)

Batali pamene zipangizo za miyala ya chilengedwe imayikidwa m’ malo mwake ndi chitsanzo cha choonadi cha uzimu. “Wankulu woposa Solomoni” masiku ano akumanga kachisi wa uzimu. Kachisi wauzimuwu akumangidwa ndi “miyala ya moyo” yomwe ikuyikidwa pamodzi ndi Yesu Nkhristu. Komanso Kachisi ameneyu akumangidwa mwachinsisi, pomwe ikuyikidwa pamodzi mwangwiro. Izi zikuchitika mwachinsisi koma mwa dongosolo la mphanvu la “chotupitsa-ngati uvangeli.”

#### CHOTUPITSA-NGATI UVANGELI

**Ndiponso anati, Ndidzafanizira Ufumu wa Mulungu ndi chiani?**

**Ufanana ndi chotupitsa mikate, chimene mkazi anatenga, nachibisa mu miyeso itatu ya ufa, kufikira unatupa wonsewo. (Luka 13:20-21)**

Ndimeyi ikusonyeza kuti ntchito ya Mulungu simapita patsogolo chifukwa cha kufuula ndi kulengeza. Mutha kumayembekezera kuti Ufumu wa Mulungu ufalitsidwa kudzera munjira za nkondo pogonjetsa mayiko ena. Koma kufalitsidwa kwa Ufumu wa Mulungu kuli nagti chotupitsa mu mkate. Chotupisa chitha kukhala chaching’ono komanso chobitsika, koma chiri ndi kuthekera kopanda malire. Ngati chotupitsa, mphanvu ya Ufumu siyakunja koma yankati mwa munthu.

Mu chitsanzo china, Yesu anayerekeza kufalitsidwa kwa Ufumu wa Mulungu ndi ka mbeu kampiru

**Pamenepo ananena, Ufumu wa Mulungu ufanana ndi ciani? ndipo ndidzaufanizira ndi ciani?**

**Ufanana ndi kambeu kampiru, kamene munthu anatenga, nakaponya m'munda wace wace, ndipo kanamera, kanakula mtengo; ndi mbalame za m'mlengalenga zinabindikira mu nthambi zace. (Luka 13:18-19)**

Mu fanizo lapitalo, Yesu anayerekeza chikhulupiriro ndi ka mbeu ka mpiru. Ananena kuti palibe chosatheka ngakhale ndichikhulupiriro chochepa. Mofanana ndi m'momwe chotupitsa chimafalikira, ka mbeu ka mpiru kamodzi kamakula ndikukhala ntengo waukulu. Chitsanzo chimenechi chimasonyeza mwa chete, koma ndi njira yamphanvu yopititsa patsogolo Ufumu.

Pali njira zambiri zatsopano zomwe zingathandidze pakufalitsa Uthenga Wabwino. Izi zimatchedwa kuti “luso lazasayansi.” Zimaphatikidza zinthu monga malo osindikizira mabuku, makina a kompyuta, wailesi zonvera ndi za kanema, zomvetsera ndi zoonera. Njira zatsopano zakayendedwe zimathandizanso anthu kuyenda mofulumira kukafalitsa Uthenga Wabwino. Luso la sayansi ndilofunikira kwambiri koma mphanvu ya Uthenga Wabwino ndiya nkati. Mwa ichi tikuthauza kuti mphanvu ili mu Uthenga Wabwino. Ichi ndi chimwene fanizo la chotupitsa ndi la mbeu ya mpiru likunena.

Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu ukachulukitsidwa kuti ukafikire “mtanda” onse wa dziko lapansi chifukwa cha mphanvu ya Ufumu imene iri ngati chotupisa mu nkate. Izi zikuonetsera kuti kufalitsidwa kwa Uthenga Wabwino suchepesedwa ku malo komwe kulibe luso la sayansi. Ngakhale ndichikhulupiriro chochepa, Ufumu wa Mulungu upitabe patsogolo. Uwu ndiwo chotupitsa-ngati uvangeli.

### **TANTHAUZO LA UVANGELI**

Mawu oti “uvangeli” akuchokera ku mawu achigiliki oti “evangelion.” Pali magawo anayi a mauwa. Liu limodzi litanthauza “uthenga wabwino,” mau awiri athathauza “kulengeza za uthenga wabwin,” ndipo lina limatanthauza “mlaliki” kapena munthu amene akulengeza.

Uvangeli si mndandanda wa mikumano kapenda utumiki wa mpingo. Uvangeli ndiwosiyana ndi chitsitsimutso. Chitsitsimutso ndi ntchito imene Ambuye akugwira mu mpingo. Mu Chitsitsimutso, chimatsindikidza kupedzeka kwa Ambuye komwe kukubwezeretsa moyo kwa anthu ake.

Uvangeli ndi mpingo omwe ukugwira ntchito ya Ambuye. Uvangeli umatsindikidza kubadwatso mwatsopano, chiyambi cha moyo wa uzimu. Kusinthika komwe kuli zotsatira chitsitsimutso, komabe zimapangitsa kuti mphanvu ya uvangeli ikhale yochitachita yomwe imabweretsa “zolengedwa zatsopano mwa Nkhristu” zomwe zikupangisa kuti zinthu ziwirizi zizikhalira limodzi mu moyo wauzimu.

Uvangeli ndi

*... “kulankhula Uthenga wabwino kudzera mwa mphanvu ya Mzimu Woyera mu njira yoti amuna ndi akadzi amakhala ndi kuthekera kolandira Yesu Nkhristu kukhala Mpulumutsi ndi Mbuye ndikukhala mamembala ofunikira a mpingo wake.”*

Tiyeni tikambirane tanthauzoli mwatsatanetsatane. Uthenga Wabwino ndi uthenga womwe ukuyenera kulalikidwa. Uthenga wofunikira wa Uthenga Wabwino waikidwa mwachidule mu 1 Akorinto 15:1-5, koma “Uthenga wabwino wa Ufumu” umaphatikidza zonse zomwe Yesu anaphunzitsa (Mateyu 28:18-20). Kusinthika kochokera mu Baiibulokumabweretsedwa ndi choonadio. Uthenga Wabwino ndikukumana kwa choonadi ndi kusalungama, nkhristu ndi ochimwa, komanso Kumwamba ndi Gehena.

Ndi Uthenga Wabwino wa ufumu wa Mulungu omwe ukuyenera kugawidwa, osati chikhalidwe cha anthu kapena zikhukupiriro za mipingo. Cholinga si kuukira dongosolo la

ndale akapena zipembedzo zina. Cholinga sikusitha anthu, koma kuona anthu akusintha chifukwa cha mphanvu ya Uthenga Wabwino.

Cholinga si “ntchito zabwino” za maphunziro, zamankhwala, kapena kusamalira komanso dongosolo lodyesa anthu. Zinthu izi ndizabwino pokwanirisa Ntchito imene Yesu Nkhristu anayisiya ngati zikuchitika molingana ndi utumiki wa Uvangeli. Kulalika Uthenga Wabwino kukuyenera kukhala cholinga chofunikira apo ayi zimangokhala zochitika zosangalatsa anthu chabe.

Yesu anatumikira kuzokhumba za anthu zakuthupi pakudyesa makamu a anthu, powachilitsa komanso kuwamatsula. Koma ntchito izi zimachitika molingana ndi uvangeli. Dzimayenda pamodzi ndi kuphunzitsa ndi kulalikirira Uthenga wabwino.

“Kulankhula Uthenga Wabwino” kukutanthauza kuti uthenga ukuyenera kufalitsidwa munjira yomwe ingapangise anthu kulandira Yesu Nkhristu ngati mpulumutsi ndi Mbuye. Ngati mungafaritse Uthenga Wabwino munjira iyi, mukupanga uvangeli.

Ngati mungapange uvangeli, mukuyenera kukhala olumikizana ndi anthu omwe atayika mu uchimo, mwaichi, uvangeli ukuyenera kuchitika ku malo omwe kuli anthu ochimwa.

“Kudzera mwa mphanvu ya Mzimu Woyera” zikutanthaudza kuti Uthenga sukuyenera kufalitsidwa ndi mau okha, komanso kudzera pakuonetsera mphanvu. Paulo anati:

**Ndipo mau anga ndi kulalikirira kwanga sanakhala ndi mau okopa a nzeru, koma m’chionetso cha Mzimu ndi cha mphanvu;**

**kutichikhulupiriro chanu chisakhale m’nzeru ya anthu, koma mu mphanvu ya Mulungu. (1 Akorinto 2:4-5)**

“Kudzera mwa mphanvu ya Mzimu Oyera” zikutanthaudzanso kudzoza kwa Mzimu Woyera kukuyenera kukhala pakufalitsa Uthenga Wabwino, pakuti zimatengera ntchito ya Mzimu kuti anthu atembenukwe ntima.

**Kulibe mmodzi akhoza kudza kwa Ine koma ngati Atate wondituma Ine amkoka iye... (Yohane 6:44)**

“Kulandira” Kutanthauza kuti wokunva wavomeredza Uthenga Wabwino. Uthenga opanda muyitano ndimalangizo chabe. Ndi chirimbikitso, osati uvangeli. Mu uvangeli weniweni, pakuyenera kuperekedwa mwayi ovomeredza. Kuperekeramboni ya momwe utatembenukira ntima ndi njira ya uvangeli yochedwa kupereka umboni, koma uwu si uvangeli. Kupera umboni sikutanthauza kupindura. Kupereka umboni ndikofunika, koma sikutsimikiza chipulumutso. Uvangeli weniweni utanthaudza kuwabweretsa anthu kwa khristu mwa njira yoti atha kuona okha ubwino opanga chisankho paokha. Zotsatira za uvangeli ndiiko kubadwatso mwatsopano komwe kumatchedwanso kuti “kutembenuka” kapena “chipulumutso.”

“Kumulandira Yesu Nkhristu kukhala Mpulumutsi ndi Mbuye” sikungotanthauza kuvomereza kulandira chipulumutso chabe, koma dongosolo lomwe limapangisa Yesu Nkhristu kukhala Mbuye wa moyo wanu. Izi zikuonetsera kuti otembenuka ntima amakhala ophunzira omwe amakhala m’bali yofunika ya mpingo. Ziwani kuti “ndi mpingo wake,” zomwe zikutanthauza kuti thupi lake la Khristu lenileni, osati mpingo wa kuthupi kapena bungwe.

“Mwayi wonveka” utanthauza kuti uthenga ukuyenera kulalikidwa mu njira yoti aliyense athe kumvetsesa. Izi zikutanthauza kuti kalankhulidwe uthanga kukuyenera kugwirizana ndi

maphunziro, ndi zikhalidwe za anthu. Izi zikuthanthauzanso kuti sitinganene kuti munthu kapena dera lapulumutsidwa chifukwa tinakalalikirako kamodzi kokha. Umboni ukuyenera kulankhulidwa mpaka anthu atamvetsesa ndi kupatsidwa mwayi oti avomereze uthenga. Anthu, banja, fuko, kapena mtundu titha kunena kuti walandira uthenga pomwe alandira Uthenga Wabwino omwe ungawapase mwayi ovomereza ndi chikhulupiriro. “mwayi onvekawu” umatanthauzanso uthenga wamphanvu omwe umapereka mwayi kuti anthu aone chionetsero chookena cha Uthenga Wabwino podzera mu machilitso ndi kumatsulidwa ku nsinga za satana.

## **KUFUNIKA KWA UVANGELI**

Ndichifukwa chani dziko lapansi likufunika uvangeli? Pofuna kuyankhu funsoli, mukuyenera kumvesetsa zinthu ziwiri: Tanthauzo ndi kothera kwa otayika.

### **TANTHAUZO LA OTAYIKA**

Muwerenge kulengedwa kwa dziko ndi munthu mu Genesis mutu woyamba ndi wachiwiri. Komanso muwerenge Genesis 3 za m'mene tchimo linalowera mu dziko. Pamene Adamu ndi Hava analengedwa, anali ndi chikhalidwe chabwino chosachimwa. Atachimwa chikhalidwechi chinasokonekera. Pamene Adamu ndi Hava anayamba kukhala ndi ana, ana obadwawo anabadwa ndi chikhalidwe chauchimo. Munthu sanalitso wabwino mungo Mulungu anamulengera. Malingaliro ndi zichitochito zake zinakhala zoipa.

Genesis 4:1-6:4 imafotokodza m'mene tchimo linafalikira pa dziko lonse lapansi. Ndime zimenezi zimakamba za kuphana koyamba, bodza loyamba, komanso m'mene kuyipa kwamunthu kunakulira mpakana malingaliro, kachitidwe kadzinthu, kanali koyipa. Dziko lapansi linakhala lochimwa mpakana Mulungu analapa kuti walenga munthu (Genesesi 6:5-6)

Chifukwa cha kukula kwa tchimo, Mulungu anaganiza zoononga Dziko lapansi ndi chigumula koma anapulumutsa munthu modzi olungama, Nowa ndi banja lake. (Muwerenge nkhani ya Nowa mu Genesis 6:8-9:17) chigumula chitatha, banja la Nowa linayamba kuchulukana. Posatenga nthawi, ntchimo linayamba kuonekera. Ichi ndichifukwa chake anthu kulikonse amatchedwa “ochimwa.”

### **Pakuti onse anacimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu; (Aroma 3:23)**

Anthu onse omwe sanalape tchimo lawo komanso sanabadwe mwatsopano malingana ndi m'mene Yesu anafotokodzera mu Yohane 3 akutengedwa “otayika” chifukwa ataya chikhalidwe chopanda uchimo chimene Mulungu anachilenga pachiyambi. Tikhodzanso kunena kuti “sanapulumutsidwe” kapena “ndiosakhulupirira” chifukwa sanapulumutsidwe ku machimo awo pakudzera pakukhulupirira mu Ambuye Yesu Nkhristu ngati Mpulumutsi.

### **MATHERO A ANTHU OTAYIKA**

Chifukwa cha kuchimwa kwa Adamu ndi Hava, imfa inalowa mu dziko ndipo chifukwa cha ichi aliyense amafa mwa thupi. Pokutha kwa imfa yakuthupi pamabwera chiweruzo.

### **Ndipo popeza kwaikikatu kwa anthu kufa kamodzi, ndipo atafa, ciweruziro. (Ahebri 9:27)**

Pakutha kwa imfa, tonse tizayima pamaso pa Mulungu kuti tikaweruzidwe. Anthu omwe sanalape tchimo lawo azakumana ndi imfa yachiwiri. Azafa “imfa yaku uzimu” yomwe izawarekanitse iwo ndi Mulungu kwamuyaya. Mathero awo ndi Hegena:

### **Pakuti mphotho yace ya ucimo ndi imfa; koma mphantho yaulere ya Mulungu ndiyo moyo wosatha wa mwa Kristu Yesu Ambuye wathu. (Aroma 6:23)**

**Ndipo ndinaona akufa, akuru ndi ang'ono alinkuima ku mpando wacifumu; ndipo mabuku anatssegulidwa; ndipo buku lina linatssegulidwa, ndilo la moyo; ndipo akufa anaweruzidwa mwa zolembedwa m'mabuku, monga mwa nchito zao...**

**Ndipo ngati munthu sanapezedwa wolembedwa m'buku la moyo, anaponyedwa m'nyanja yamoto. (Cibvumbulutso 20:12,15)**

Ukanvetsetsa mathero a iwo otayika, umadzindikira kufunika kwa uvangeli. Ngati anthu safikiridwa ndi Uthenga Wabwino, azafa mu uchimo nakathera ku Gehena wamuyaya.

## **NDONDOMEKE YA UVANGELI**

Uvangeli ndi ndondomeko yomwe imaphatikidza kupezeka komanso kulengeza za Uthenga Wabwino, kukopa, kubzala, ungwiro, ndi kutengapo gawo. Tiyeni tione ndondomekodzi:

### **KUPEZEKA:**

Uvangeli wa “kupedzeka” ndikumene kumaonetsera ubwino wa Yesu pakuonetsera makhalidwe a Chikristu. Dziko lapansi silingafikiridwe ndi Uthendga wa Yesu Khristu ngati Akhristu sapezeka mokhulupirika. Ukhulupirira akuyenera kuphunzira kumanga ubale, komanso kuthandidza osakhulupirira. Sungakope ochimwa ngati ngati ulibe ubale wabwino ndi ochimwawo.

### **KULENGEZA:**

Okhulupirira ambiri amakhala Ackhristu “achinsisi.” Amaganiza kuti kupezeka kwawo pakati paosakhulupirira ndikokwanira kukwanirisa Utumiki Waukulu yolalikira dziko. Koma lamulo la Yesu ndilakuti tikuyenera kulankhula Uthenga Wabwino podzera kulalika, kuphunzisa, ndi kuchitira umboni. Komanso tikuyenera kuwonets mphanvu ya Uthenga Wabwino kudzera kumachilitso ndi mamatsulidwe. Umu ndi m'mene uthenga umalengezedwera.

### **KUKOPA ENA:**

Kulalikira Uthenga Wabwino sikuthesa ndondomeko ya uvangeli. Uthenga Wabwino ukuyenera kuperekedwa mu njira yomwe anthu angakopedwe kuti akhale okhulupirira mwa Yesu Khristu.

### **KUBZALA:**

Otembenuka atsopano omwe akopedwa kutsata Yesu akuyenera “kubzalidwa” mu mpingo kapena mpingo ukuyenera “kubzalidwa” pakati pa magulu a okhulupirira atsopano.

### **UNGWIRO:**

Zotsatira za kubzalidwa, otembenuka amakula muuzimu pomwe kulanga kukukwaniritsidwa malingana ndi mpingo omwe iwo ali. (Kukula muuzimu kumatchedwa “ungwiro” mu Baibulo)

### **KUTENGA NAWO GAWO:**

Uvangeli umakwaniritsidwa ngati okhulupirira atsopano akugwira nawo ntchito ya uvangeli nayamba kubereka mu uzimu.

## MAYESO OZIYESA NOKHA

1. Lembani mavesi otsogolera

---

2. Tanthauzani “chotupitsa-ngati uvangeli”

---

3. Kodi “tanthauzo la otayika” imanthauzanji?

---

4. Kodi “tsogolola otayika” litanthauzanji?

---

5. Lembani masitepe asanu ndi imodzi a ndondomeko ya uvangeli

---

---

---

---

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)



## ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Mu phunziro loyambayi mwaphunzira tanthauzo la “uvangeli”

**Uvangeli:** Uvangeli ndi kulankhula Uthenga wabwino kudzera mwa mphanvu ya Mzimu Woyera mu njira yoti amuna ndi akadzi amakhala ndi kuthekera kolandira Yesu Nkhristu kukhala Mpulumutsi ndi Mbuye ndikukhala mamembala ofunikira a Mpingo Wake.

Nawo mawu ena omwe mukuyenera kuwadziwa:

### **Uvangeli kapena Kulalikira:**

Mau awa amagwiritsidwa ntchito pochita ntchito ya uvangeli.

### **Kulalikiidwa**

Anthu, banja, fuko, kapena mtundu titha kunena kuti walandira uthenga pomwe alandira Uthenga Wabwino omwe ungawapase mwayi ovomereza ndi chikhulupiriro. Ndongomeko ya thunthu ya uvangeli imaphatikidza ubzala otembenuka mu mpingo kapena, kubzala mpingo pakati pa magulu a aokhulupirira atsopano.

### **Mlaliki**

Mlaliki ali ndi mphatso yotsogolera yapaderadera yochokera kwa Mulungu yomwe ili kuthekera kogawana Uthenga Wabwino ndi osakhulupirira munjira yomwe amuna ndi akadzi amavomereza ndi kukhala mamembala odalirika mu thupi la Khristu. Mau oti “mlaliki” amatanthauza kuti “obweresa uthenga wabwino.” Ingakhale okhupupirira onse alibe mphatso yapaderadera yotsogolera ya mlaliki, onse akuyenera kugwira ntchito yolalika.

### **Kuchitira Umboni**

Okhulupirira kumuza osakhulupirira m'mene anakumanirana ndi Yesu Khristu.

### **Uvangeli wa Panokha**

Uvangeli wa panokha ndi munthu okhulupirira kulankhula Uthenga Wabwino kwa munthu osakhulupirira.

### **Mtsonkhano wa uvangeli:**

Mtsonkhano wa uvangeli umatchedwanso uvangeli wa “gulu”. Ndi kulankhula Uthenga Wabwino kwa gulu la anthu. Limaphatikidza zochita ngati misonkhano yachitsitsimutso ndi zoyimbayimba za Uthenga Wabwino.

### **Uvangeli wa wamba:**

Mawu awa amatanthauza ntchito ina iri yonse ya uvangeli yachitidwa ndi anthu wamba (anthu omwe alibe maudindo okhazikika mumpingo).

### **Uvangeli wolowerera:**

Uvangeli wolowerera uthanthauza “kulowerera” ku malo onsendicholinga choti munthu wina aliyense afikiridwe ndi Uthenga Wabwino.

### **Kutembenuka:**

Otembenuka ndi munthu yemwe wavomeredza Yesu Khristu ngati Mpulumutsi. Watembenuka kuchokera ku moyo wake kakale wa uchimo kupita ku moyo watsopano mwa Yesu.

### **Ophunzira:**

Ophunzira ndi otembenuka amene wakhazikika mu chikhulupiriro cha chiKhristu ndipo ali ndikuthekera kokuza otembenuka atsopano ndi kumawaphunzisa. Mau oti “ophunzira” amatanthauza kuti munthu yemwe akuphunzira potsatira.

### **Kutsatira Otembenuka:**

Kutsatira otembenuka ndi ndondomeko yophunzisa otembenuka atsopano ndikuwabweretsa ku kukhwima mwa Khristu, zomwe zikutsatira kukhazikika kwa uzimu, kukula, ndi kubalana. Izinso zimatchedwa kuti “kuphunzisa” chifukwa zimatantahuza kutega otembenuka atsopano ndikuwapanga kukhala ophunzira a Ambuye Yesu Khristu.

2. Mu nthawi ya Chipangano Chakale, Mulungu anamuza Abrahamu kuti kudzera mwa iye mitundu onse ya dziko lapansi lidzadalitsika. Koma dalitsi linabwera ndi udindo waukulu. Abrahamu amayenera kutuluka m’dziko lake, kwa abale ake, ndi ku nyumba ya atate ake kunka ku dziko lomwe Mulungu azamutsonyeze iye (Genesis 12:1)

Poyamba Abrahamu anapita ku malo lotchedwa Harana ndi kukhala kumeneko (Genesis 11:31). Anayetsedwa kukhala ku Herana, koma kuti alandire m’dalitso amaenera kumvera Mulungu ndi kuchoka ku malo ameneri. Abrahamu sanakakhala tate wa mfuko lalikulu ndi kukwaniritsa zokhumba za ntima wake pa nthawi imodzi. Kudutsa malire a mzinda wa Harana ndi kuchokako kuti akakwaniritse zolinga za Mulungu chinali chiganizo chopambana chomwe Abrahamu anapanga.

Kodi mukudziwa kuti ndinu okhulupirira lero chifukwa cha chiganizo cha Abrahamu? Chifukwa choti Abrahamu anatuluka mu Harana, Mulungu anamudalitsa. Kudzera mwa Abrahamu, anthu amitundu yonse kuli konse ndi odalitsika ndi Uthenga Wabwino. Ndiodalitsika chifukwa chipulumutso chodzera mwa Yesu Khristu chinacholekera mu banja la Abrahamu chifukwa cha kumvera kwake.

Ngati Abrahamu. Mukalandira m’dalitso mumalandiranso udindo waukulu. Kwa wo omwe adalitsika ndi chipulumutso ndi Mzimu Woyera, uvangeli si chisankho. Ndi udindo (Machitidwe 1:8).

Kukamba mwa uzimu, okhulupirira aliyense amakumana ndi “Harana” mu moyo. “Harana” wauzimuyu ndi malo omwe Mulungu amafunsa, “kodi muli okonzeka kusiya zokhumba za ntima wanu kamba ka chifukwa cha Uthenga Wabwino? Muli okonzeka kutuluka ku dziko lakwanu, kwa abale anu, kunyumba ya atate anu ndikakufunsani kutero?” simungakwaniritse zokhumba zanu ndi kudalitsa mitundu pa nthawi yomweyo. Mukuyenera kudutsa malire ndi kutsiya Harana kumbuyo.

3. Baibulo likuta “Cotupitsa pang'ono citupitsa mtanda wonse” (Agalatiya 5:9). Mwaphunzira muphunzirori kuti Ufumu wa Mulungu umachulukitsidwa ngati chotipitsa. Zoipa nazonso zimachulukitsidwa mu njira yomweyi. Werengani mavesi ostaticirawa: Mateyu 16:6-12; Marko 8:15; 1 Akorinto 5:6-8. Mu Chipangano Chatsopano, chotupista chimakamba za chikhslidwe cholowa paliponse cha Uthenga Wabwino kapena mpatuko (makhalidwe obwerera m’mbuyo) a mpingo. Mu Chipangano Chakale, chotupitsanso chinali ndi tanthauzo lomwelo. Sichimaloledwa mu zopereka zina, pomwe chimaimirira zoipa, koma mu zopereka zina, monga zopereka zamayamiko, chimaloledwa.

4. Ngati muli m'busa kapena tsogoleri mu mpingo waku dera lanu, mugwiritse ntchito mafunso otsatirawa kuti muyese m'mene uvangeli uliri mu mpino wanu. Mulembe mayamkho anu pa pepala lina lapadera:

- (1) Kodi yemwe ali ndi udindo wopanga mapulani (chikonzero) cha uvangeli ndi ndani?
- (2) Kodi ndi anthu angati omwe anatembenuka ndi kukhala mbali imodzi ya mpingo wanu mu dzaka zisanu zapitadzi?
- (3) Kodi mpingo wanu ukuchitapo chani kuti mukafikire anthu osapulumsidwa? Muyankhe mwachindunji.
- (4) Kodi ndi mapologalamu ati omwe mpingo wanu uli nawo omwe sakuthandiza pa uvangeli ndi kubala otembenuka atsopano?
- (5) Kodi mpingo wanu ukuchitapo chani pofuna kuthandiza ma membala ake kuti adzindikire mphatso za uzimu zomwe ali azo ndikuzigwiritsa ntchito pa ntchito ya uvangeli?
- (6) Kodi mpingo wanu uli ndi chinodzero chotani chofuna kufikira m'mudzi wanu ndi Uthenga Wabwino?
- (7) Kodi mpingo wanu uli ndi chikonzero chotani chofikira mtundu wanu ndi Uthenga Wabwino?
- (8) Kodi mpingo wanu uli ndi chikonzero chotani chofikira mitundu ina ndi Uthenga Wabwino?
- (9) Kodi ndi nthawi zochuluka bwanji zimene mpingo wanu wapereka maphunziro apaderadera a uvangeli kwa mamembala anu?
- (10) Kodi ndi nthawi zofuluka banji zimene pologalamu yanu mpingo imakamba za unangeli, mwa chitsanzo mautheenga ofuna kuti mukafikire osapulumsidwa, kupereka mwayi kuti anthu avomereze Uthenga Wabwino, ndi zina zambiri.
- (11) Kodi ndi liti limene mpingo wanu unatengapo gawo pa uvangeli wa gulu, kupangitsa msokhano, kapenena mayimbidwe, ndi zina zambiri.

**Wunikirani mayankho anu pakulingalila zotsatilazi:**

- (1) Ngati mulibe munthu yemwe amapanga chikonzero cha uvangeli mu mpingo wanu, kodi simukuganiziira zosankha munthu?
- (2) Ngati chiwerengero cha anthu omwe anatembenuka ndi kukhala mbalali ya mpingo mu dzaka zisanu zapitazo ndi chochepe, kodi izi zingasinthidwe bwanji potsindika za uvangeli?
- (3) Kodi mpingo wanu ungapange chani chamwangu kuti mukafikire osapulumsidwa?
- (4) Kodi ndi ma pologalamu anji osabala zipatso omwe mpingo wanu ukuchita panopa omwe atha kuchotsedwa kuti akapereke mwayi ku mapologalamu ena atsopano, okhuza uvangeli?
- (5) Kodi mpingo wanu umgathandize bwanji kuti mamembala azindikire mphatso zawo zauzimu ndi kuzigwiritsa ntchito pa uvangeli? (Phunziro la Harvestime International Institute course la "Njira Zosonthanitsira" itha kukuthandizani)
- (6) Kodi mpingo wanu ungayambe kuchita chani kuti ukafikire mudzi lanu ndi Uthenga Wabwino?
- (7) Kodi mpingo wanu ungayambe kuchita chani kuti ukafikire mtundu lanu ndi Uthenga Wabwino?
- (8) Kodi mpingo wanu ungayambe kuchita chani kuti ukafikire mitundu ina ndi Uthenga Wabwino?
- (9) Kodi mpingo wanu uyamba liti maphunziro apaderaddera a uvangeli kwa mamembala anu? (Mutha kugwiritsa ntchito phunziro iri pakuwaphunzisa ma membala anu. Mukonze nthawi yoyenera ndi amene angazaphunzise)

- (10) Kodi mungafikire bwanji osapulumsidwa mu chipembedzo chanu ndi kuwapatsa mwayi oti avomwreze Uthenga Wabwino?
- (11) Kodi mpingo wanu ungapange chani ku malo omwe kukuchitikira uvangeli wag ulu? Kodi mungapange dongosolo la nsonkhano wa chipulunutso kapena mayimbidwe kapena mutha kugwirizana ndi mipingo ina kuti mupange msonkhano wa chitsitsimutso?

## CHAPUTALA 2

### LAMULO

#### ZOLINGA

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba vesi yotsogolera.
- Kupeza mfundo zisanu zomwe lamulo la uvangeli lakhazikikapo.
- Kupeza zinthu zitatu zofunikira pokwaniritsa lamulo la uvngeli.

#### VESI YOTSOGOLERA:

**Ndikati Ine kwa woipa, Woipawe, udzafa ndithu, osanena iwe kumcenjeza woipayo aleke njira yace, woipa uyo adzafa m'mphulupulu yace, koma mwazi wace ndidzaufunsa pa dzanja lako. (Ezekieli 33:8)**

#### CHIIYAMBI

Anthu amatenga mbali pa uvangeli pazifukwa zosiyanasiyana. Anthu obadwa mwatsopano kumene amakhala ochitachita pa uvangeli chifukwa amakhala osangalala ndikutembenuka ntima kwawo. Anthu ena amakaamizika kupanga uvangeli chifukwa cha kutsutsidwa ntima kwawo. Ena chifukwa maphunziro omwe akupanga amawafunsa iwo kutero.

Chifukwa cha m'malemba chomwe tikuyenera kutengapo gawo pa uvangeli ndi chifukwa choti ndi lamulo lochokera kwa Ambuye Yesu Khristu. “lamulo” ndi ntchito imene imaperekedwa kuchoka kwa munthu modzi kupita kwa wina. Lamulo la uvangeli ndi mutu wa nkhani mu phunziro iri.

#### LAMULO LA UVANGELI

Lamulo lomwe linaperekedwa ndi Ambuye Yesu Khristu kupita kwa omutsatila ake lakhazikika pa mfundo zisanu zomwe zikuphunzidwa mu Mau a Mulungu. Izi ndi mfundo za kulamula, maonekedwe, kukhudzidwa, mpikisano, ndi chimaliziro.

#### LAMULO:

Uvangeli wakhazikika pa mfundo za lamulo. Uvangeli walamuidwa ndi Yesu mu m'ndime zambiri zimene zikudziwika kuti “utumiki waukulu.” Zitsanzo zotsatirazi zikukhuzana ndi lamulo la uvangeli. Ndime zonse zikukamba za ntchito, koma mosiyana. Sizikutsutsana, koma zikukuthandizana pakuwonetsa mbali zosiya za lamulo.

Mateyu ndi Yohane analemba ulamuliro wa ntchito ya uvangeli. Mateyu, Marko, ndi Luka akufotokoza za mlingo wa ntchito. Mateyu, Luka, Yohane, ndi Machitidwe akuonetsera Mzimu Woyera ngati mphanvu yotahanziza pokwaniritsa ntchito. Marko anakamba za uthenga ndipo Luka anafotokoza mwatsatanetsatane. Maumboni awa akuwonetsera kuti lamulo la uvangeli limaphatikidza kupanga ophunzira, kulalika Uthenga Wabwino kwa zolengedwa zonse, kulalikira kulapa ndi kuchotsedwa kwa machimo kwa dziko lonse, kukhulukira machimo ndi kuchitira umboni wa Yesu.

**Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera:**

**Ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya pansi pano. (Mateyu 28:19-20)**

**Ndipo ananena nao, mukani ku dziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse.**

**Amene akhulupirira nabatizidwa, adzapulumutsidwa; koma amene sakhulupirira adzalangidwa.**

**Ndipo zizindikilo izi zidzawatsata iwo akukhulupirira; m'dzina langa adzaturutsa ziwanda; adzalankhula ndi malankhulidwe atsopano;**

**Adzatola njoka, ndipo ngakhale akamwa kanthu kakufa nako, sikadzawapweteka; adzaika manja ao pa odwala, ndipo adzacira. (Marko 16:15-18)**

**Ndipo anati kwa iwo, Kotero kwalembedwa, kuti Kristu amve zowawa, nauke kwa akufa tsiku lacityatu;**

**Ndi kuti kulalikidwe m'dzina lace kulapa ndi kukhululukidwa kwa macimo kwa mitundu yonse, kuyambira ku Yerusalemu.**

**Inu ndinu mboni za izi. (Luka 24:46-48)**

**Cifukwa cace Yesu anatinso kwa iwo, Mtendere ukhale ndi inu; monga Atate wandituma Ine, Inenso ndituma inu.**

**Ndipo pamene anati ici anawapumira, nanena nao, Landirani Mzimu Woyera.**

**Zocimwa za anthu ali onse muwakhululukira, zikhululukidwa kwa iwo; za iwo amene muzigwiritsa, zagwiritsidwa. (Yohane 20:21-23)**

**Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezere ace a dziko. (Macitidwe 1:8)**

kufunika malamulowa kukutsimikiziridwa mu ma vesi otsatirawa:

**Ndikati Ine kwa woipa, Woipawe, udzafa ndithu, osanena iwe kumcengeza woipayo aleke njira yace, woipa uyo adzafa m'mphulupulu yace, koma mwazi wace ndidzaufunsa pa dzanja lako. (Ezekieli 33:8)**

**Pakuti amene ali yense: adzacita manyazi cifukwa ca Ine ndi mau anga, Mwana wa munthu adzacita manyazi cifukwa ca iye, pamene adzafika ndi ulemerero wace ndi wa Atate, ndi wa angelo oyera. (Luka 9:26)**

## **MAONEKEDWE:**

Lamulo la uvangeli limaoerekedwanso chifukwa cha maonekedwe a zokolola za m'munda wa dziko lapansi. Timaona mazana mazana a anthu omwe atayika mu uchimo, opanda chiyembekezo, akupita ku muyaya opanda Mulungu. Maonekedwe awa atioangitse ife kuti tichitepo kanthu. Yesu anati zokolola zacha, koma ogwira ntchito ndiochepa:

**Ndipo ananena kwa iwo, Dzinthu dzicuruka, koma anchito acepa; potero pemphani Mwini dzinthu, kuti akankhe anchito kukututa kwace. (Luka 10:2)**

**Kodi simunena inu, kuti, Yatsala miyezi inai, ndipo kudza kumweta? Onani ndinena kwa inu, Kwezani maso anu, nimuyang'ane m'minda, kuti mwayera kale kufikira kumweta. (Yohane 4:35)**

#### **KUKHUDZIDWA:**

Lamulo la uvangeli limakhazikikanso pa mfundo ya kukhudzidwa. Uvangeli ukuyenera kuchitika ndi ntimawa chifundo pa miyoyo yotayoka. Paulo anadzadzina ndi chifundo cha umuulungu pa otayika. Anali okonzeka kutsutsidwa ndi Mulungu iye mwini chifukwa cha abale ake achi Yuda kuti apulumutsidwe. Anapitabe kwa iwo ngakhale anamuopseza kuti amupha ndi pomwe anavutika m'manja mwao.

Chifundo cha Yesu chinamupangisa kukhala ofuna kukumana ndi ntanda wa kavale. Yesu analira chifukwa cha kusaona kwa akuluakulu achipembedzo amu Yerusalemu. Tinakakhala ndi mitsonzi yambiri yachifundo mwa ife, mwina munakakhala kulira kochepe mu Gehena pa otayika. M'tsutso siungapulumutse otayika. Wina atha kukhala ndi choonadi, komangati sichilankhulidwa mu chikondi ndi muchifundo chipha m'malo molimbikisa.

Chifundo chimapangisa kuti anthu asatope ndi uvangeli, chifukwa chikondi chimapirira, chikwirira zinthu zonse, ndipo sichitha nthawi zonse (1 Akorinto 13:4,7,8). Chikondi ichi chachifundo chimaperekedwa ndi Mzimu wa Mulungu. Ndi chipatso cha Mzimu Woyera chomwe chimakula ndi kupedzeka kwake kwa Iye nkati mwanu.

#### **MPIKISANO:**

Lamulo la uvangeli imakhadzikikanso pa mfundo za mpikisano. Ngati sitikhala ndi chipambano pa abale athu omwe ali ndi njala ya kusintha, zipembezo zina zomwe tili nazo pa mpikisano zipambana. Njala ya uzimu limapangisa anthu kusaka choonadi:

**Koma ngati Mzimu wa iye amene adaukitsa Yesu kwa akufa akhalabe mwa inu, iye amene adaukitsa Kristu Yesu kwa akufa adzapatsanso moyo matupi anu akufa, mwa Mzimu wace wakukhala mwa inu. Cifukwa cace, abale, ife tiri amangawa si ace a thupi ai, kukhala ndi moyo monga mwa thupi. (Aroma 8:11-12)**

Ingakhale kuti njala ya uzimu imapangisa anthu kusaka choonadi, itha kupangitsa kulandira miyambo yoyipa, ndi mphanvu zipembedzo zoponderedza ngati njalayi sinakwaniiritsidwe.

Mfundo za mpikitsano zinaphunzitsidwa ndi Yesu mu fanizo lomwe m'dani anakabzala nansongole mu m'munda wa zokolola. Ngati sitibzala ndi kukulitsa mbeu zabwino za Mau a Mulungu, m'dani abzala nansongole. Ndi mpikitsano wa minga za uzimu ndi nansongole omwe umatsamwitsa Mau a Mulungu ndi kulepheretsa kufalitsidwa kwa Uthenga Wabwino.

#### **CHIMALIZIRO:**

Lamulo la uvangeli limakhadzikikanso pa chimaliziro cha zinthu. Yesu anati kufalikira kwa uvangeli pa dziko lonse lapansi ndi chiyambi cha kubweranso kwa Iye pano pa dziko ndi kutha kwa nthawi ngati momwe tikudziwira:

**Ndipo uthenga uwu wabwino wa Ufumu udzalalikidwa pa dziko lonse lapansi, ukhale mboni kwa anthu h mitundu yonse; ndipo pomwepo cidzafika cimariziro. (Mateyu 24:14)**

## **M'MENE MUNGAKWANIRITSIRE LAMULO**

Mpingo ndiwohandidzira Ufumu wa Mulungu pa dziko ndipo unalamulidwa kupititsa Uthenga Wabwino kwa anthu onse a padziko. Tikamaona zinthu zofunika, mapologalamu, ndi zochitika za pa mpngo matsiku anao, titha kumadabwa kuti mwina tayiwala kapena tasongonekezeka ndi ntchito yathu ngati okhulupirira.

Tiri otanganidwa, komakutanganidwa ndikuchita chani? Kodi ndi mapologalamu athu angati, mikumano yathu, ndi zochititka zomwe zimabweretsa otembenuka? Tili ndi azilaliki achionetsero ndi maualiki apamwamba odzadza ndi nkhani zoseketsa. M'Baibulo, ulaliki umodzi wokha unapangitsa anthu zikwi zitatu kutembenuka ntima. Matsiku ano zimaonetsa kuti tiri ndi maualiki zikwi zitatu ndi zotsatira zochepe chabe.

Pali njimbo za zbwino za chipembedzo, zomwe zambiri zimangoonetsa luso la anthu ayimba. Koma kodi ndi miyoyo ingati yomwe imatembenuka ntima? Kodi ndi miyoyo ingati chomwe imasintha? Tikaonjezera ku zikwi zikwi za Akhristu omwe ndi achithupi opanda kukhudzidwa ndi zokolola za uzimu, titha kufunsapo, “Kodi ntchito ya uvangeli izakwaniritsidwa liti?”

Zinthu zitatu ndizofunikira ngati tingafune kukwaniritsa lamulo la uvangeli:

### **UKUYENERA KUKHALA OYAMBIRIRA:**

Uvangeli ukuyenera kukhala oyambirira pa china chilichonse. Tikuyenera kuyika ntchito yopititsa Uthenga Wabwino kwa munthu aliyense pa dziko lapansi kukhala patsogolo. Maulaliki athu, mapemphero, mapulani, mapologalamu, kaphunzitsidwe--chilichonse chikuyenera kukhadzikika ma cholinga chimenechi.

Mpingo ukuyenera kukhala malo otumidzi anthu kupita kukalalika osati malo opumirako kapena kotsangalalirako. Zochitika zilizonse zapamlingo zikuyenera kulunjika kubweretsa pamodzi anthu opindula miyoyo. Akuluakulu a mpingo akuyenera kukhala obweretsa pamodzi Thupi la Khristu, kulimbikitsa ndi kuphunzitsa okhulupirira kuchita ntchito ya uvangeli.

### **IKUYENERA KUPATSIDWA MPHANVU NDI MZIMU WOYERA**

Uvangeli mu Chipangano Chatsopano siunachitidwe mopanda mphanvu. Ndi kukumana nndi mphanvu pakati pa Mzimu Woyera ndi mphanvu ya zoipa. Mzimu Woyera ndi zipatso zake zonse, mphatso, ndi mphanvu, akuyenera kukhala weniweni mu miyiyo yathu. Mau akuyenera alalikiidwe ndi kuphunzitsidwa ndi kaonetseredwe ka mphanvu. Chuma cha mphatso inaliyiyonse ya uzimu cha membala wina aliyense wa Thupi chikuyenera kusonkhanitsidwa kuti chikakwaniritse ntchito ya uvangeli. Tikuyenera kusinthanisa chikhalidwe chatu chakuthupi ndi chikhalidwe chofanana ndi Khristu chomwe chingatithandize ife kuchitira umboni wa choonadi wa Uthenga Wabwino.

### **UKUYENERA KUTSATIRA KACHITIDWE KA CHIPANGANO CHATSOPANO:**

Ngati tikufuna kukwaniritsa lamuloli, tikuyenera kulenganso kachitidwe ka uvangeli ka n'Chipangano Chatsopano. Aliyense, kulikonse, tsiku ndi tsiku kuchitira umboni ndi kupindula miyoyo. Monga ngati mu nthawi za Chipangano Chatsopano, uvangeli ukuyenera kukhala mbali imodzi ya moyo wathu watsiku ndi tsiku. Mpingo uliwonse, m'tsogoleri aliyense, nyumba iliyonse, ndi munthu wina aliyense akuyenera kutsankhanidzidwa kuti akagwire ntchito.



## MAYESO OZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera

---

2. Lembani mfundo zisanu zimene lamulo la uvangeli lakhazikikapo.

---

---

---

3. Pezani zinthu zitatu zofunikira kuti tikakwaniritse lamulo la uvangeli.

---

---

---

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

## ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Muyitano wa uvangeli si malingaliro kapena chinthu choti munthu usankhe. Ndi lamulo. Onani tchati yomwe iri m'musiya ndipo muyiyerekedze ndi zolembedwa zosiyanasiyana za utumiki waukulu. Muone m'mene zafotokodzedwa mu Baibulo lanu. Zindikirani ulamuliro omwe mukuyenera kukwaniritsa pa lamulo. Tsatani mlingo wa utumiki wanu, uthenga wake, ndi muzochitika zomwe mukuyenera kuchita nawo pa kachitidwe ka kachulutsidwe.

Malembo	Ulamuliro	Mlingo	Uthenga	Zochitika
Mateyu 28:18-20	“Ulamuliro onse”	Mitundu yonse	Zinthu zonse Yesu analamulira	Kuphunzisa mu ubatizo, chiphunziso
Marko 16:15	Dzina la Yesu	Dziko lonse, zolengedwa zonse	Uthenga Wabwino Chizani odwala	Pitani ndi Kalalikireni
Luka 24:46-49	Dzina la Yesu	Dziko lonse kuyambira ku Yerusalemu	Kulapa ndi kukhulukiridwa kwa machimo	Kulalikira, kulengeza, ndi Kuchitira umboni
Yohane 20:21	Kutumizidwa ndi Yesu monga Anatumizidwira ndi Atate	(Mlingo wa utumiki, uthenga, ndi zochitika ndi zofanana ndi “za Yesu”)		
Machitidwe	Mphamvu ya Mzimu Woyera	Yerusalemu, Yudea, Samaliya, ndi kulalekezero a dziko lapansi	Khristu	Kuchitira mboni

2. Kupatsidwa lamulo la uvangeli a m'Mau a Mulungu, kodi ndichifukwa chani Akhristu ambiri amazengereza kukwaniritsa utumiki waukulu? Nazi zolepheretsa za uvangeli:

### KUPANDA LUSO:

Anthu ambiri samapanga uvangeli chifukwa amaona ngati alibe luso loyenera. Atha kusowa maphunziro kapena chidziwitso cha Baibulo ndi njira za uvangeli. Ena sasowa luso, koma ali ndi chithunzithunzi cholakwikwa kapena kuzichepesa konyenga.

Nthawi zonse mudzikumukira kuti Mulungu amaitana anthu owoneka opanda mphanvu kukachita zinthu zakuya. Muwerenge nkhani ya Gidiyoni pa Oweluza 6 mpaka 8. Pamene Gidiyoni anayitanidwa kukakwaniritsa utumiki waukulu ya Mulungu, anabitsala chifukwa amaopa adani ake. Yankho lake linali loti “kodi ndingapange bwanji izi?” ntundu wanga ndi woluluka (opanda mphanvu) ndipo ine ndiri wang'ono mu banja langa.”

Mose naye anayankha ngati chomwechi pamene anayitanidwa kukatsogolera mtundu wa Israyeli. Anati “Ndine yani? Ine ndine munthu wosowa ponena, kapena dzulo, kapena kale, kapena chilankhulire Inu ndi kapolo wanu, pakuti ndine wa m'kamwa molemera, ndi wa lirime lolemera” (Eksodo 4:10). M'neneri Yeremiya anadzinenera kuti iye ndi mwana ndipo siwoyenera kugwiritsidwa ntchito ndi Mulungu (Yeremiya 1:4-9).

Anthu omwe anaonangati alibe luso la uvangeli akuyenera amufunse Mulungu nzeru zimene analinjeza (Yakobo 1:5). Akuyenera kunvetsesa kuti Mulungu amagwiritsa nthito iwo omwe alibe luso lobadwa nalo kuti alandire ulemu onse (1 Akorinto 1:27-29)

### **KHAMA LOSAFUNIKIRA:**

Anthu ambiri samapanga kalikonse chifukwa amaona ngati kuti khama lawo likhala losafunikira chifukwa zokolola zoti zitutidwe ndizambiri. Kodi munthu m'modzi angakwanise kulalikira ku miyanda miyanda ya anthu otayika? Mukukumbukira kuti gulu la nkhangongo la Gidiyoni linachepetsedwa ndicholinga choti Mulungu akalandire ulemu m'malo mwa munthu (Oweruza 7). Mulungu amakondwera ndikutenga khala losafunikira ndi kuligwiritsa nthito ku zolinga zake. Muphonzira muphonzirori m'mene munthu modzi, kupindura ndi kuphonzitsa munthu m'modzi pachaka, zingakwanitse kuzutsa zikwizikwi za okhulupirira pa nthawo yochepe. Nyali imodzi singathese m'dima pa iyo yokha, koma tinyali tambiri, yatsani imodzi pa nthawi, kenako mupanga kuwala kwakukulu.

### **MANTHA:**

Anthu amaopa kuti akanidwa ndi iwo omwe akuwachitira umboni. Ngati sakudzindikira njira za uvangeli, amaopa chinthu chomwe palibepo. Amaopa kuti achittsidwa manyazi ndi nyengo zomwe sangakwanitse kuzisamalira kapena mafunso omwe sangakwanitse kuyankha. Mantha a uvangeli nthawi zonse amayambira pa mafunso awa:

-Kodi ndikalankhula chani? Muphonzira za uthenga omwe mungakapereke mu Mutu wa Chitatu wa phonzirori.

-Ndichilankhule bwanji? Muphonzira m'mene mungakankhulire uthenga mu Mutu wa Chisanu wa phonzirori

-Kodi ndingathane nawo bwanji mavuto? Mutu wachi Khumi wa phonzirori ukukamba za m'mene mungathanire ndimavuto omwe angadze pamene mukuchita uvangeli.

-Bwanji ndikalephera kuyankha funso? Ngati simungathe kuyankha funso, vomerezani. Muuzeni munthuyo kuti mukawerengenso za funsola ndipo mubweranso kwa iye.

-Bwanji ndikakhumudwitsa wina? Zomwe zimakhumudwitsa anthu zikuyankhula mwa tchutchuchu za Mulungu, koma kunamizira kuti muli ndi mayankho onse, nkwiyo, kapena mikangano. Ngati muli achikondi ndi oona ntima mukachitidwe kanu ka zinthu ndipo anthu akukhumudwitsikabe, kumbukirani kuti: Ndinu nchere wa dziko lapansi. Mu dziko lakuthupi, nchere ukatikidwa pachilonda umapangitsa machitidwe osasangalatsa poyamba, koma umachiritsa. Izinso ndi m'mene ziriri mu dziko lauzimu.

-nanga bwanji ndikalephera? Ndibwino kuyetsera ndi kulephera kusiyana ndikusayetseratu. Kuchita bwino ndi kulephera si nkhwana zikuluzikulu za uvangeli. Inu mwaitanidwa ku kukhulupirira. Mitundu itatu ya kulephera yalembedwa mufanizo la ofesa (Marko 4:1-20). Mu phonzirori, Marko atiuza kuti ndi nthaka, lokodzedwa ndi Mzimu Woyera, imene imabala mbeu, osati ofesa. Izi zisagwiritsidwe nthito ngati chothawirapo kuti tipewe anthu kuti azizipereka. Tinayitanidwa kuti tikaweze miyoyo ya anthu osati kungowakopa chabe.

### **KUDZIPATULA:**

Uvangeli umalepheretsedwa chifukwa sitimalumikidzana ndi osakhulupirira. Ngati abwenzi anu onse ndi Akhristu, simukwanitsa kupindula otayika. Simungawafikire osakhulupirira ngati simumalumikidzana nawo.

## **OSAKWANIRA**

Nthawi ndi zolimbikitsa zosakwanira zimarepheretsa anthu kukwaniritsa lamulo la uvangeli. Nthawi zonse kumbukirani, komabe... Mumapedza nthawi kuchita zomwe mukufuna muchite ndi zomwe mukuona kuti ndizofunikira. Ngati mulibe nthawi yogawa Uthenga Wabwino, ndiye kuti simukufuna kugawa kapena mukuona kuti ndizosafunikira. Mukuyenera muonetso zofunikira zanu. Kusowa chilimbikitso kumabwera chifukwa cha kusowa kwa zokumana nazo m'moyo. Kodi munadzindikira m'mene Akhristu atsopana amakhalira okondwa kugawa chikukhupiriro chawo? Izi ziri chomwechi chifukwa zomwe zinawachitikira zikadali zatsopano ndi zotsangalatsa. Mukapanga kusamala, mukutha kwa nthawi mumataya izi ngati simusunga ubale wabwino ndi Ambuye.

## **KUSAKHWIMA MU UZIMU:**

Paulo anawauza okhulupirira kuti azitha kuphunzsa Uthenga Wabwino kwa anthu ena, koma chifukwa cha kusakhwima mu uzimu samakwanisa chichita izi (Ahebri 5:12). Kusakhwima mu uzimu kumaonetseredwa pomwe Akhristu sakunvana okhaokha (1 Akorinto 3:1-3). Ngati mukutaya nthawi kumenyanana ndi n'Khrisu nzanu, sumuakhala ndi nthawi yochita uvangeli.

3. Pano ndipo mwaphunzira zifukwa zimene zimalepheretsa uvangeli, werengati ziganizo zotsatirazi ndipo muone zomwe zikufotokodza kanvesedwe kanu:

## **KUSOWA LUSO:**

- \_\_\_ Sindikudziwa kuti ndinena chani.
- \_\_\_ Sindikumvetsesa Baibulo bwinobwino.
- \_\_\_ Sindimakwanitsa kulankhula ndi anthu ena.

## **KHAMA LOSAFUNIKIRA:**

- \_\_\_ Ndikumva kuti sindingasithe zinthu chifukwa ndiripo ndekha.
- \_\_\_ Nthcito ya uvangeli ndiyochuluka.

## **MANTHA:**

- \_\_\_ Ndiri ndi mantha kuti ndikhumudwitsa ena.
- \_\_\_ Ndiri ndi mantha nditha kulephera.
- \_\_\_ Ndiri ndi mantha sindidziwa m'mene ndingayankhire mafunso.
- \_\_\_ Ndiri ndi mantha ndichititsidwa manyazi.
- \_\_\_ Sindikudziwa chonena.

## **KUDZIPATULA:**

- \_\_\_ Ndiribe kulumikidzana kulikonse ndi osakhulupirira.

## **OSAKWANIRA:**

- \_\_\_ Ndiribe nthawi ya uvangeli.
- \_\_\_ Ndiribe chilimbikitso cha uvangeli.

## **KUSAKHWIMA MU UZIMU:**

- \_\_\_ Sindimamva kuti ndine okhwima mu uzimu kuti ndikagawe Uthenga Wabwino kwa anthu ena.
- \_\_\_ Nthawi zambiri ndimakhala ndi vuto ndi Akhristu anzanga.

4. Wunikiranu zinthu zomwe zakambidwa mwambamo. Kumbali kwa chinthu chirichonse lembani m'men mngathanire ndi zolepheretsa podzera mu maphunziro, kuchita ma pulakatisi, mapemphero, kapena kusingha zinthu zomwe ziri zofunikira kwa inu.
5. Kodi zinthu zomwe ziri mwambamu zimene ziri zolepheretsa kwa inu ndi ziti? Kodi mungathane nazo bwanji?

## CHAPUTALA 3

### UTHENGA

#### ZOLINGA

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba ma vesi otsogolera.
- Kutanthauzira “Uthenga Wabwino wa Ufumu”
- Kulemba mwachidule zinthu zofunikira za Uthenga Wabwino.
- Kulemba zinthu zinayi zosonyeza kuti Uthenga Wabwino ndi wa dziko lonse lapansi
- Kufotokoza chifukwa chimene Uthenga Wabwino uli wa mphamvu.

#### MA VESI OTSOGOLERA

**Pakuti ndinapereka kwa inu poyamba, cimenenso ndinalandira, kuti Kristu anafera zoipa zathu, mongamwa malembo;**

**Ndi kuti anakidwa; ndi kuti anakitsidwa tsiku lacinatu, monga mwa malembo. (Akorinto 15:3-4)**

#### CHIYAMBI

Mulungu ali ndi malingaliro apaderadera pofuna kufikira dziko lonse lapansi ndi Uthenga wabwino. Yesu anavumburutsa malingaliro amenewa pomwe adawaudza ophunzira ake:

**... Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezere ace a dziko. (Macitidwe 1:8)**

Vesi iyi ikuonetsera zinthu zambiri zokhudza uvangeli:

-Yesu Kristu ndiye chidzalo cha uthenga.

-Ophunzira ndi otengera Uthenga Wabwino omwe akwaniritsidwa ndi mphamvu ya Mzimu Woyera

- Dziko lonse ikukhala cholandira uthenga

Mu phunziro iri muphunzira za chidzalo cha uthenga. Mu Mutu lachinayi muphunzira za atumiki a Uthenga Wabwino amene ali okhulupiriro omwe apatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera. Mutu Lachisanu ikukamba za anthu omwe ali ndi uthenga m'mene angalankhulire uthenga ndipo Mutu Lachisanu ndi Chimodzi likukamba za anthu omwe akulangira uthenga.

#### UTHENGA WABWINO WA UFUMU

Yesu anati:

**Ndipo uthenga uwu wabwino wa Ufumu udzalalikiwa pa dziko lonse lapansi, ukhale mboni kwa anthu h mitundu yonse; ndipo pomwepo cidzafika cimariziro. (Mateyu 24:14)**

Uthenga wa Uvangali ndi Uthenga Wabwino wa Ufumu. Mau oti “Uthenga” ukutanthauza “uthenga wabwino.” Tikamakamba za Uthenga Wabwino mu malembo a m'baibulo, umatanthauza uthenga wabwino wa Ufumu wa Mulungu komanso chipulumutso kudzera mwa Yesu kristu.

Pa Aroma 1:1 Uthenga ukutchedwa kuti “Uthenga Wabwino wa Mulungu.” Pa Aroma 2:16 ukutchedwa kuti “Uthenga Wabwino wa Paulo.” Pa Aroma 1:16 ukutchedwa kuti “Uthenga Wabwino wa Khristu.” Ndime zimenedzi sizikuzitsutsa zokha chifukwa Mulungu ndiye olemba Uthenga Wabwino, Khristu ndiye mutu waukulu, ndipo munthu ndiye ali olandira Uthenga.

### ZINTHU ZOFUNIKA ZA UTHENGA WABWINO

Pa 1 Akorinto 15:1-4, zinthu zofunikira za Uthenga Wabwino zaperekedwa ndi Paulo:

**Ndipo ndikudziwitsani, abale, Uthenga Wabwino umene ndinakulalikirani inu, umenense munalandira, umenense muimamo,**

**Umenense mupulumutsidwa nao ngati muugwiritsa monga momwe ndinalalikira kwa inu; ngati simunakhulupira cabe.**

**Pakuti ndinapereka kwa inu poyamba, cimenense ndinalandira, kuti Kristuanafera zoipa zathu, mongamwa malembo;**

**Ndi kuti anaikidwa; ndi kutianaukitsidwa tsiku lacityatu, monga mwa malembo. (1 Akorinto 15:1-4)**

Uthenga ofunika kwambiri wa Uthenga Wabwino ndiwo kuti Kristu anafa chifukwa machimo athu monga mwa malembo, anaikidwa ndi kuti anaukitsidwa kwa akufu monga mwa malembo. Uthenga Wabwino utha kufupikitsidwa pa uthenga wa pa Yohane 3:16

**Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha. (Yohane 3:16)**

Tanthauzo la Uthenga Wabwino limaphatikidza zonse zomwe Yesu anawaphunzitsa ophunzira ake:

**Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse... ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu... (Mateyu 28:19-20)**

Anthu akuyenera kuti audzidwe za Ufumu, alimbikitsidwe kuti alowem'mo, komanso aphunzitsidwe m'mene angakhalire ngati anthu okhalamo.

Uthenga Wabwino womwe timalalikira siuthenga wachikhalidwe wofuna kusintha dera, koma Uthenga Wabwino wa Mulungu omwe cholinga chake ndikupulumutsa anthu ochimwa. Uthenga wa Ufumu ukuyenera kuyitana anthu kuti akalape machimo awo.

**Ndipo ataperekedwa Yohane, Yesu anadza ku Galileya, nalalikira uthenga wabwino wa Mulungu,**

**Nanena, Nthawi yakwanira, ndipo Ufumu wa Mulungu wayandikira; tembenekani mtima, khulupirani uthenga wabwino. (Marko 1:14-15)**

(Ngati simunanvetsese zolinga za Ufumu wa Mulungu, pedzani phudzilo la Harvestime International Institute la “*Makhalidwe a Ufumu.*”)

### UTHENGA WA DZIKO LONSE

Mau ofunikira kwambiri omwe ali mu Uthenga Wabwino ndi mau oti “yense.” Anagwiritsidwa ntchito ndi Yesu (Yohane 3:16), Paulo (Aroma 10:13), komanso Yohane

(Chibvumbulutso 22:17). Uthenga Wabwino ndiwakwaanhu onse amitundu yonse, komanso maiko onse. Ndi uthenga wa dziko lonse pa zifukwa zinayi

1. Tchimo ili pa dziko lonse: Aroma 3:23
2. Chipulumutso chaperekedwa ku dziko lonse: 1 Timoteo 2:4
3. Lamulo loti anthu alape machimo ndira dziko lonse: Machitidwe 17:30
4. Mayitanidwe kuti anthu akhulupirire ndi a dziko lonse: Aroma 10:9-11

### **MPHAMVU YA UTHENGA WABWINO**

Muli mphamvu mu UthengaWabwino. Paulo adati:

**Pakuti Uthenga Wabwino sundicititsa manyazi; pakuti uti mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa munthu ali yense wakukhulupira; kuyambira Myuda, ndiponso Mhelene.**

**Pakuti m'menemo caonetsedwa cilungamoca Mulungu cakucokera kucikhulupiriro kuloza kucikhulupiriro: monga kwalembedwa, Koma munthu wolungama adzakhala ndi moyo ndi cikhulupiriro.**

**Pakuti mkwiyo wa Mulungu, wocokera Kumwamba, uonekera pa cisapembedzo conse ndi cosalungama ca anthu, amene akanikiza panso coonadi m'cosalungama cao;**

**Chifukwa codziwika ca Mulungu caonekera m'kati mwao; pakuti Mulungu anacionetsera kwa iwo. (Aroma 1:16-19)**

Mavesi zimaonetsera chifukwa chimene Uthenga Wabwino uli wa mphamvu. Uli wamphanvu chifukwa:

- Ndi chibvumbulutso cha mphamvu ya Mulungu kwa munthu
- Umabweretsa chipulumutso kwa anthu onse, osatengera ntundu wa anthu, khungu, kapena chikhulupiriro.
- Umabvumulutsa chimene chikuyenera kudziwidwa ndi anthu chokhudzana ndi Mulungu
- Umabvumulutsa chilamulo komanso nkwiyo wa Mulungu pa tchimo
- Umabvumbutsa chilungamo cha Mulungu
- Umaonetsa mmene anthu amalungamitsidwira (kukhulukiridwa kwamachimo, kubwezeretsedwa mu ubwenzi wabwino ndi Mulungu) mwa Chikhulupiriro
- Ndi maziko a chikhulupiriro omwe ife timakhalapo.

### **KAONETSEREDWE KA MPHAMVU**

Uthenga Wabwino ukuyenera kulalikidwa ndi kuphunzitsidwa, komanso ukuyenera kuonetsera machitachita a Ufumu wa Mulungu. Yesu anawaudza omutsatira ake kuti:

**... pamene mulikupita lalikani kuti, Ufumu wa Kumwamba wayandikira.**

**Ciritsani akudwala, ukitsani akufa, konzani akhate, turutsani ziwanda: munalandira kwaulere, patsani kwaulere. (Mateyu 10:7-8)**

Uthenga wa Ufumu si uli m' mau okha chabe. Kuonetseredwa kwa mphamvu kukuyenera kuperekedza kulalikira kwa mau. Izi zinatsimikdziridwa ndi chitsanzo chimene Yesu anayika:



**Ndipo Yesu anayendayenda m'mizinda yonse ndi m'midzi, namaphunzitsa m'amasunagoge mwao, nalalikira uthenga wabwino wa Ufumuwo, naciritsa nthenda iri yonse ndi zofoka zonse. (Mateyu 9:35)**

**Koma unyinji wa anthu, pamene anadziwa, anamtsata Iye; ndipo iye anawalandira, nalankhula nao za Ufumu wa Mulungu, naciritsa amene anasowa kuciritsidwa. (Luka 9:11)**

Kuonetsera kwa mphamvu, zozizwa komanso machiristo ndi kuchitachita kwa Ufumu wa Mulungu. Izizikuyenera kukhala mbali imodzi ya uthenga wa uvangeli. Paulo adati:

**Pakuti ufumu wa Mulungu suli m'mau, koma mumphamvu. (Akorinto 4:20)**

## MAYESO OZIYESA NOKHA

1. Lembani ma vesi otsogolera

---

---

---

2. Tanthauzirani “Uthenga Wabwino wa Ufumu”

---

---

3. Kodi zinthu zofunikira za Uthenga Wabwino ndi ziti?

---

---

4. Lembani zinthu zinayi zosonyeza kuti Uthenga Wabwino ndi wa dziko lonse lapansi

---

---

---

5. Fotokozani chifukwa chimene Uthenga Wabwino uli wa mphamvu.

---

---

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

## ZOONJERA POPHUNZIRA

1. Kuti muphunzire zambiri za Ufumu wa Mulungu, mupezw phunziro la Harvestime International Institute lotchedwa “*Kukhala mu Ufumu.*”
2. Muwerenge 2 Mafumu 4:29-37. Iyi ndi nkhani yomwe m’men Elisa anaukusa mwana ku akufa. Muyewere chiyambi cha nkhanayi pa 2 Mafumu 4:8-17. Mwana uyu anali mwana wa chozizwa, yemwe anaperekedwa ku yankho la pemphero la Eliya ndi chopempha cha mzimayi waku shunemu yemwe anamuonetsera mneneri chifundo. Nkhani yonse ya kufa kwa mwana yaperekedwa mu ma vesi a 18-20. Chomwe chinapangisa kuti mwana afe sichinaperekedwe. Zitha kukhala kuti zinachokera ku mtundo wina wa sitiroko (matenda akufa ziwalo) chifukwa manayo amadandaula za mutu wake. Nkhanayi ndi chitsanzo chimene choonadi cha uzimu pokamba za uvangeli chikhoza kuonedwa. Uvangeli uli ngati kuukisa wakufa chifukwa mumapulumsa anthu kuchokera ku imfa ya uzimu yamuyaya. Baibulo limati moyo omwe umachimwa uzafa, pakuti mphoto ya uchimo ndi imfa, ndipo ochimwa amafa mu zolakwa ndi uchimo. Ntchito ziri m’musimu zitha kupezedwa kuchokera mu nkhani ya 2 Mafumu 4. Kuukisa akufa:

### I. Mukuyenera kukhala ndi chikhulupiriro:

- A. (Mavesi 20-21) Mzimayi wa mwana sanangovemereza imfa ya mwana wake. Pachizolowezi amayenera kuyamba kulira, kuyitana ogwira ntchito yolira, ndikuyamba kukodza thupi kuti ikayikidwe kumanda.
- B. M’ malo mwake, (vesi 21) anamugoneka pakama la Elisa, natseka chitseko, ndipo anapita kutantenga m’neneri. Kuti mumvetsetse izi, mukuyenera kuwerenga nkhani ya pa 1 Mafumu 17:17-24 pomwe Eliya anaukitsa mwana kuchokera kwa akufa. Kutenga mwana kupita naye mu chipinda cha m’meneri anali machitidwe a chikhulupiriro pokumbukira chozizwa chomwe Eliya anachita. Sanadikirire kuti m’meneri amutengere nkati. Anamutengera yekha, ndikumadikirira chozizwa chofanana.
- C. Mulungu wakhala akuukitsa akufa kuyambira pachiyambi. Tiwatenge anthu osapulumuka, m’mene aliri, ku malo achozizwa.
- D. (mavesi 22-23) Muone chikhulupiriro chake pomwe anayankha funso mwamuna wake. “kuli bwino.”
- E. Mukayamba kumachita pa chikhulupiriro, chimachuluka. Pa nthawi yomwe anali atafika pafupi ndi m’meneri, chikhulupiriro chake chinakula. (Vesi 26) Pomwe Elisa anantuma wantchito wake Gehazi kukanfunsa mafunso, sanayankhe kuti “kuli bwino.” Anati “ali bwino.”

### II. Mukuyenera kukhala wofulumira: Pa vesi 22 mkaziyo anati: “kuti ndithamangire.”

Mukuyenera kukhala wofulumira pakuukisa akufa chifukwa miyoyo ikufa tsiku ndi tsiku.

### III. Mukuyenera kudula chikhalidwe

- A. (Vesi 23) M’mamuna wake anamufunsa, “Ukumuka kwa iye lero chifukwa chani?” sichinali chikhalidwse chake chomapita kwa m’mneneri. Ngati mwezi wakhala, kapena mpa sabata.
- B. Mukuyenera kudala chikhalidwe kuti mukapanga evangeli wa kuwonetsera mphamvu. Anthu atha kuuuza kuti, “izi si njira zomwe timapangira zinthu.”

### IV. Mukuyenera kukhala wachifundo:

- A. (Mavesi 25-27) Akufa sakaukitsidwa ndi a “Gehazi” omwe alibe chifundo. Pamene mkaziyo anadza kufunafuna moyo, analibe chifundo ndipo anakatha kumubwenza.
- B. M’neneri anaonensa kukhuzidwa. Anafutsa, “Muli bwino kodi? Mwamuna wanu ali bwino? Mwanayo ali bwino?”

- C. Pali anthu amene avutika kuti atipeze ife. Amadzunzika ndikugwa pa mapazi athu, komabe timapawonya kunja. Timawatumidza ku azilangizi achikunja, amakhwala ozunguza ubongo, kapena ku malo okonzaso moyo.
- V. Mukuyenera kupita komwe ali:
- A. (Vesi 29-31) Kuti muthandize iwo omwe ali akufwa mu uchimo, mukuyenera kupita komwe al ngati m'mene Elisa anapitira kwa mwanayo.
- B. Sitingatumize anthu opanfa mphamvu (ngati Gehazi) kapena kusitha miyeso (yaimiriridwa ndi ndodo). Kuti akatiukise ife kwa akufa, yese anadza padziko lino lapansi. Anadza komwe ife tiri.
- C. Mzimayi sanakhazikike pa zinthu zolowa mmalo. Anthu akufa sangafune chinachirichonse chosiyana ndi mphamvu ya Mulungu yomwe iri yokwanitsa kupupira m'peya wa moyo mu moyo wawo wakufa.
- D. Pamane mkaziyo ananena chokhumba chake, Elisa poyamba anatumiza Gehazi kuti akatumikire kwa mwanayo. Koma, wakufayo sanaukitsidwe ndi "Gehazi" --ngakhale Gehaza ananyamula ndodo ya Mulungu. Gehazi anapita mofulumira kuposa Elisa ndi mzimayiyo, nakayika ndodo pa mwanayp, koma panalibe yankho.
- E. Ngati mukufuna kuukitsa akufa, mukuyenera kutsatira chitsanzo cha mbuye wathu. Muwerednge 1 Mafumu 17:17-24. Eliya, amane anali mbuye wa Elisa, anasiya chitsanzo choukutsa mwana wakufa. Anakakhala kuti Elisa anatsata chitsanzochi, sanakatumiza Gehazii ndi mdodo yake kuti akayesere kugwira ntchito.
- F. Elisa amaona ngati mphamvu ya Mulungu ikagwira ntchito ngakhale iye kulibeko ndi khama lake. Timatenga ziphunziso za mpingo ndikkuzigoneka pa omwe ali akufa ku uzimu, koma ife sitifuna kutengapo gawo. Timayesera njira zosiyanasiyana kupaula ife kutengapo gawo, koma sitikhala ndi chipambano pa moyo wakufu ngati mdodo ya Elisa.
- G. Kalata ya chilamulo yopanda Mzimu siyingaukitse anthu akufa. Moyo suwungayende ngati akuluakulu akuyika manja ndi ndodo osayanjanitsika pa amuna ndi akadzi.
- VI. Mukuyenera kudzindikira chidzalo cha vuto:
- A. (Vesi 31) Gehazi sanakhulupirire kuti mwanayo anali atafa. Anakanena kuti "sanauke mwanayo." Mwanayo sikuti anali akugona. Anali atafa. Gehazi samakhulupirira ndipo analankhula ngati kuti wangogona.
- B. (Vesi 32) Elisa amadziwa kuti mwanayo wafa.
- C. Osakhulupirira omwe atayika mu uchimo sikuti angogona. Ndi vuto lalikulu ndithu. Ndi imfa ya uzimu, ndipo saukitsidwa pokhapokha titadzindikira izi.
- VII. Mutsagonjetsedwe ndi kulephera:  
(Vesi 31... "mwanayo sanauke.") Kuyetsera koyamba koukitsa mwana kunalephereka. Mukalephera pakuyesa koyamba, mutsatsiye. Mutsamatsurire kulephera kwanu kuti simutayitanidwe ku ntchito. Phunziro la kulephera sikuyisa kugwira ntchito, koma kusintha njira. Mukuyenera kutsatira njira za mbuye wathu.
- VIII. Mukuyenera kuukitsa wakufa mu nchipida chankati:  
(Vesi 33) Mukuyenera kupita mu "nchipida cha nkati" cha pemphero, mutseke chitseko, ndi kuyamba kupempherera anthu omwe akufa mu chimo.
- IX. Mukuyenera kuvekedwa ndi mphamvu:
- A. Pomwe amalowa mu nchipinda cha nkati, Elisa anadziwa kale komwe kumachokera mphamvu zake. Pa nthawi ina izi zisanachitike, chobvala cha Eliya chinagwera pa iye. Anadziwa kochokera mphamvu zake. Inayetsedwa ndi kuvomeredzedwa.
- B. Mwa inu nokha, simungabweretse mitima yokufa ya anthu ku moyo. Mulungu ndikochokera mphamvu zanu. Chobvala cha Mzimu Woyera chinagwera pa ndi kubatizidwa kwa mphamvu.
- X. Mukuyenera kudziwa zolinga:

Cholinga chanu sikuti mukasambitse thupi lakufa, ndi kuyikonza ndi mafuta onunkhir. Izi zonse ndizongopititsa patsogolo, koma mudakali ndi thupi lokufa. Cholinga chanu sikuphunzisa makhalidwe, kuzipititsa patsogolo kwa munthu mwini, kuvindikira uchimo, kapena kusintha dera. Cholinga chanu ndi moyo watsopano wauzimu.

XI. Mukuyenera kukhala wa moyo.

- A. Vesi 34 imatsonyeza kuti thupi la mwanayo linayamba kufunda. Koma Elisa sanangokhazikika pa chidzindikiro ichi. Si anthu ofunda omwe tikufuna, koma moyo. Osati zakunvainva, koma chitsitsimutso chenicheni.
- B. Elisa anayendayenda, nadikirira ndi osakayika anayitanira pa Mulungu. Ndipo anadzitambasuliranso pa mwanayo. Pa nthawi iyi, mwanayo anayetsemula kasanu ndi kawiri. (Mau oti “uyetsemula” amatanthauza “kupuma”). Pomwe anapuma, watsopano unalowa m’nthupi lake, ndipo anatsegula maso anke mwanayo. Pomwe anthu akufa akupuma mphamvu yokhudza ndi yokonzaso ya “m’phepo ya mphamvu yothamanga ya Mzimu Woyera,” iwonso adzakumana ndi moyo watsopano omwe ukuyenda kuchokera ku mphamvu yachiukitsa ya Mulungu.

## CHAPUTALA 4

### OTUMIKIRA

#### ZOLINGA

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba vesi yotsogolera.
- Kulemba mwachidule gawo la Mau a Mulungu pa Uvangeli
- Kufotokoza udindo wa Mulungu pa uvangeli.
- Kuzindikira gawo la Yesu pa uvangeli.
- Kulemba mwachidule gawo la Mzimu Woyera pa uvangeli.
- Kufotokoza gawo la pemphero pa uvangeli.
- Kuzindikira gawo lanu mu uvangeli.
- Kutanthauza mau oti “umboni”
- Kutanthauza mau oti “anthu wamba.”
- Kutanthauza mau oti “m’busa.”
- Kufotokoza chomwe chikutanthauza pakuyitanidwa kwa anthu wamba.

#### VESI YOTSOGOLERA

**Pakuti Uthenga Wabwino sundicititsa manyazi; pakuti uti mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa munthu ali yense wakukhulupira; kuyambira Myuda, ndiponso Mhelene. (Aroma 1:16)**

#### MAU OYAMBA

Mukuphunzira malingaliro a Mulungu a uvangeli kuti dziko lonse likafikiridwe ndi Uthenga Wabwino monga zabvumbutsidwira pa Machitidwed 1:8:

- Yesu Kristu ndiye chidzalo cha uthenga.
- Ophunzira ndi otumikira Uthenga Wabwino omwe akwaniritsidwa ndi mphamvu ya Mzimu Woyera.
- Dziko ndi choloandira uthenda.

Mu phunziro lathali mwaphunzira za chidzalo cha Uthenga Wabwino. Mu phunziro iri muphunzira za otumikira uthenga. Mau a Mulungu, Mulungu Tate, Mwana komanso Mzimu Woyera, ndi pemphero onse pamodzi amaphatikidza mphamvu zawo za uzimu kuti otumikira Uthenga Wabwino akachite umboni wa mphamvu wa Uthenga Wabwino.

#### MAU A MULUNGU NDI UVANGELI

Uthenga Wabwino uli ndi mphamvu mwa iwo okha okwaniritsa kubadwanso kwa uzimu mwa moyo omwe ukulandira uthenga.

**Pakuti Uthenga Wabwino sundicititsa manyazi; pakuti uti mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa munthu ali yense wakukhulupira; kuyambira Myuda, ndiponso Mhelene. (Aroma 1:16)**

Sumukuyenera kukhala ndi mphatso ya ulaliki kuti mukhale otumikira Uthenga Wabwino. Chomwe chiri chofunika ndikufalitsa Uthenga Wabwino omwe mwa iwo okha umapulumsa munthu.

Ukamafalitsa Mau a Mulungu, chikhulupiriro cha anthu omwe akunvera uthenga sichikhala pa nzeru zanu kapena luso lanu lakaperekedwe ka uthenga (1 Akorinto 2:5). Komanso mutha kukhala otsimikidzidwa kuti Mau a Mulungu sabwerera osagwira ntchito yake. Amakwaniritsa cholinga cha Mulungu (Yesaya 55:11). Mau amatulutsa kaonetseredwe ka mphamvu ka zizindikiro ndi zodabwitsa zomwe zimakopa osakhulupirira za choonadi cha Uthenga Wabwino (Marko 16:20).

### **GAWO LA MULUNGU PA UVANGELI**

Mulungu ndi amene amasintha moyo wamunthu kudzera pakubadwanso matsopano. Mutha kuchitira umboni, kulalikira, komanso kuphunzitsa Uthenga Wabwino mwa kuthekere kwanu konse, koma ndi Mulungu yekha yemwe amasintha moyo wa munthu. Mukanvetsetsa izi, nkhawa zanu zonse zomwe mumakhala nazo pa uvangeli zimatha.

Inu ndinu otumikira chabe, zotengera za kuthupi zogwiritsidwa ntchito ya umulungu. Ndizosatheka kuti inu mukasinthe munthu. Kubadwanso mwatsopano kumachokera kwa Mulungu. Pamene munthu wabadwanso mwatsopano, ndi “obadwa mwa Mulungu”:

**Yense wokhulupirira kuti Yesu ndiye Kristu wabadwa kucokera kwa Mulungu; ndipo yense wakukonda iye amene anabala akondanso iye amene anabadwa wocokera mwa iye. (1 Yohane 5:1)**

### **GAWO LA YESU PA UVANGELI**

Yesu ndiamene anapereka lamulo la uvangeli komanso anatuma Mzimu Woyera kuti akakukonzekeretseni inu ku ntchito. Ndiamene amachita nawe natsimikiza ndi zizindikiro ndi zozizwitsa.

**Ndipo iwowa anaturuka, nalalikiraponseponse, ndipo Ambuye anacita nao pamodzi, natsimikiza mau ndi zizindikilo zakutsatapo, Amen. (Marko 16:20)**

### **GAWO LA MZIMU WOYERA PA UVANGELI**

Mu nthawi ya Chipangano Chatsopano, Mzimu Woyera mabweretsa khwimbi la anthu kwa otumikira Uthenga Wabwino. Kodi tingafotokoze bwanji za anthu omwe amatsatira utumiki wawo? Kunalibe manyuzipepala, mawailesi kapena malonda a pakanema m'matsiku amenewo.

M'malo momagwiritsa ntchito njira za dziko lapansi pofuna kukopa anthu, tikuyenera kutenga nthawi yathu namakhala munzipinda za pa mwamba ngati m'mene Mpingo wakale unkachitira mpaka nafe, tivekedwe ndi mphamcu yochokera kumwamba. Ndi Mzimu Woyera womwe umatsutsa anthu nawakopa iwo zaubwinno wa chipulumutso. Njira za uvangeli zimene zayetsedwa ndizabwino pakufalitsa Uthenga Wabwino, koma Mulungu sakufuna kuti inu mudzidalira zimenezo. Mukuyenera kudalira mphamvu ya Mzimu Woyera imene imatsutsa anthu.

**Koma ndinena Ine coonadi ndi inu; kuyenera kwa inu kuti ndicoke Ine; pakuti ngati sindicoka, Nkhosweyo sadzadza kwa inu; koma ngati ndipita ndidzamtuma iye kwa inu.**

**Ndipo atadza Iyeyo, adzatsutsa dziko lapansi za macimo, ndi za cilungamo, ndi za ciweruziro. (Yohane 16:7-8)**

Ndi mphamvu ya Mzimu Woyera imene imapereka mphamvu (kuthekera) ku uvangeli. Ophunzira anali othechera, ochitira umboni ochitachita pomwe anakumana ndi mphamvuyi (Machitidwe 1:8 ndi Mutu wachiwiri).

## PEMPHERO NDI UVANGELI

Palibe chinthu mu dziko la uzimu chigapite patsogolo popanda pemphero. Ngati okhulupirira, ndinu m'modzi wa Thupi la Khristu otumidzidwa kwa otayika komanso dziko lokufa kutimukafalitse Uthenga Wawino. Koma thupi lauzimu limatsogozedwa, kulamulidwa komanso kupatsidwa mphamvu ndi mutu, omwe umagwira ntchito ngati thupi la munthu lomwe limatsogozedwa ndi mutu.

Monga momwe thupi lamunthu limayenera kukhala lolumikidzidwa bwino ku mutu ndi ziwalo zonse za thupi zolumikizana bwino, thupinso lauzimu likuyenera kulumikidzana ndi mutu wauzimu, Ambuye Yesu Kristu. Kulumikidzanaku kumachitika pakudzera nkupemphera.

Mwa njira ina: Yesu ndi mpesa ndipo ife ndi nthambi komwe dzipatso zimaberekedwa. Yesu ndi thunthu komanso m'sitsi omwe umapereka moyo ku nthambi. Chithunzithunzichi chikuonesa kudalirana. Iye amadalira ife kuti tikabereke dzipatso, ife timadalira iye pa moyo wauzimu komanso mphamvu (Yohane 15). Ubale uwu sungakhalepo popanga kulumikidzana bwino pakati pa inu ndi Ambuye. Pali chitsanzo cha ichi mu nkhani yapa Mateyu 17:14-21. Ophunzira anakanika kutumikira kwa nyamata wachichepere chifukwa chotsowa pemphero. Pemphero zimayenera kuchitika kumayambiriro kwa ntchito kokha, pemphero ndiye ntchitoyo.

Pemphero likuyenera kuchitika uvangeli usadayambike. Pa Luka 10:1-24, Yesu adawauza ophunzira ake kuti apemphere (ndime 2), kenako adawaudza kuti anyamuke (ndime 3). Pemphero limayamba kupita kusanachitike. Ndipo kutero tikapemphera mochulukwa tipindulanso miyoyo yochulukwa. Pa Machitidwe 2 adapemphera kwa masiku khumi, ndikulalika kwa mphindi khumi, anthu zikwi zitatu adapulumutsidwa. Koma lero, timapemphera kwa mphindi khumi, kulalikirira masiku khumi, ndipo anthu ochepa okha amapulumuka.

Kupemphera kwa “uvangeli” kumatanthauza kuti mukupempherera:

- (1) Ogwira ntchito mu m'munda (Luka 10:2).
- (2) Uthenga Wabwino kuti “akathamange” (2 Atesalonika 2:1-2). “kuthamanga” kumatanthauza kufalikira ponseponse.
- (3) Mwayi: pa Akolose 4:3, Paulo anafutsa kuti amupempherere kuti Mulungu “atsegule makomo a mau” kuti akagawe Uthenga Wabwino.
- (4) Kulimba ntima: Paulo anafutsa Mpingo waku Aefeso kuti umupempherere kuti agawe Uthenga Wabwino molimbika.
- (5) Chipulumutso: ndiza m'malembo kupepherera aku kuti apulumutsidwe. Aroma 10:1 imakonetsa Paulo anapempherera a Israyeli kuti apulumutsidwe.
- (6) Ntendere: Pa 1 Timothy 2:1-4, Paulo akutiudza kuti tipempherere iwo omwe ali pa mipando ya udindo kuti tikhale m'moyo wa ntendere. Ananena izi pakuti Nchokoma ndi cholandirika pamaso a Mulungu amene “afuna anthu onse apulumuke.” Uthenga Wabwino umafala mofulumira pa nthawi ya mntende pamene sukuletsedwa ndi mazunzo, nkondo, ndi zina zambiri.

Kupambana kochepa, kukhoza kutsatira khama lathu lopanda pempherero, koma khama lathu limakhala lochepa ku dzimene tinakapeza tinakhala kuti tikudzindikira kufunika kwa pemphero.



## UDINDO WANU MU UVANGELI

Otumikira Uthenga Wabwino ndi obadwatso mwatsopano. Dongotsolo la Mulungu ndiloti ophunzira aliyense akuyenera “kuchitira umboni” za Uthenga Wabwino. “kuchita umboni” ndikuuza anthu ena zomwe mwaona, mwanva, komanso mwadutsamo.

Mu chipinda chowerudziramo milandu, ochitira umboni ndiyemwe amachitira umboni wa munthu kapena chinthu. Ngati ochitira umboni, mukuyenera kuchitira umboni za Yesu komanso cholinga chake cha chipulumutso cha anthu onse. Pali mitundu iwiri ya umboni. Oyamba ndi umboni wa mau. Umboni wina ndi umboni wooneka ndi maso. Mzimu Woyera amakuthangatani inu kuti mukachitire umboni kudzera m’mau komanso kudzera mukaonetsedwe ka mphanvu ya Mulungu.

### KUSIYANA PAKATI PA ANTHU OTHANDIZA NDI AZIBUSA

Chifunira cha mulungu ndichoti ophunzira wina aliyense akachitire umboni wa Uthenga Wabwino. Mpingo oyambaa unakura pomwe umatsata chifuniro chimenechi. Okhulupirira aliyense amafalitsa Uthenga Wabwino komanso ndikubereka zipatso za uzimu. Pamene Mpingo umakula, Mulungu anaitana ena kuti akakhale azibusa, a vangeli, aneneri, aphunzitsi ndipo ena atumwi. Pakutha pa nthawi, okhulupirira amakhala m’bali imodzi ya kusiyana kuwiri kwa Mpingo. Amakhala azibusa kapena azitumiki.

Mau oti kutumikira amachokera ku mau a chi Greek omwe atanthaudza kuti “anthu osankhidwa a Mulungu.” Tanthaudzo la mauwa ndi “anthu onse a Mulungu.” Mau oti kutumikira anayamba kugwiritsidwa kwa anthu omwe samatuikira nthawi zonse mu mpingo. Mau oti m’busa anakhadzikitsidwa kuti akaonetsere mautumiki a mu mpingo. Azibusa ndi iwo amatenga utumiki ngati ntchito yawo kapena omwe alembedwa ntchito ndi mpingo.

Pakutha kwa nthawi mu mbiri ya mpingo, kusiyana kunayamba kukula pakati pa azibusa ndi azitumiki. Azitumiki ambiri anasiya kupindulira mpingo ku uzimu. Anayamba kusiyira ntchito yofikira dziko lonse kwa iwo ogwira ntchito mu mpingo. Palibe yemwe angakwaniritse ntchito yonse yimene mpingo inapasidwa yofikira dziko lonse lapansi ndi uthenga. Ichi ndichifukwa chimodzi chomwe chikupangitsa kuti titsafikirebe dziko lonse ndi Uthenga Wabwino. Baibulo limaphunzisa kugawana ntchito mu Mpingo, koma aliyense akuyenera kutengapo gawo pofaritsa Uthenga Wabwino (Machitidwe 6:1-6).

Pamene mpingo waku Yerusalemu umakula, kugawana kwa ntchito kunafunikira ndicholinga chofuna kukwaliritsa kufikira zofunikira zonse zamumpingo. Azitsogoleri anadzipereka okha ku utumiki wa mau ndi m’kupemphera. Ndipo atumiki amagwira ntchito ngati kutumikira amasiye komanso ntchito zina zothandiza. Koma ngakhale okhulupirira amagwira ntchito zosiyanasiyana mu mpingo, onse pamodzi amafalitsa uthenga Wabwino:

- Stefano anali modzi mwa atumiki omwe anasankhidwa kugwira ntchito yotumikira, komabe anaperekera umboni wamphanvu wa Uthenga Wabwino (Machitidwe 6:8-11)
- Filipo anali otumikira winanso yemwe anasankhidwa. Afalitsa Uthenga Wabwino ku Asamaliya (Machitidwe 8:5-12)
- Pomwe kuzunzika kwa mpingo kunayamba ku Yerusalemu okhulupirira anathawira m’madera ena, iwo anapitirira kuchitira umboni za Uthenga Wabwino (Machitidwe 8:4). Kwa okhulupirira eneieni, plibe kusiyana kwa osankhidwa ndi achikunja pakuti Yesu ndi Ambuye wa onse.

## **KUYITANIDWA KWA ATUMIKI**

Ngati mumanvetsetsa mayitanidwe auzimu a atumiki mukuyenera kupita ku Chipangano Chakale. Dongosolo la Mulungu linali loti ntundu onse wa Israyeli kukhala ansembe kapena otumikira.

**Ndipo ndidzakuyesani ufumu wanga wa ansembe, ndi mtundu wopatulika...  
(Eksodo 19:6)**

Ngati ansembe, munthu aliyense wa Israyeli amayenera kukhala ochitira umboni Mulungu modzi woona kwa iwo osakhulupirira omwe ali nawo limodzi. Kukhadzikitsidwa kwa ntundu wa ansembe sikunasinthe dongosolo la Mulungu pa Israyeli. Ansembe anali ngati azibusa alero omwe ali ndi utsogoleri wapaderadera. Koma dziko lonse limayenera kukhala lotumikira uthenga wa Mulungu kwa anthu amitundu.

Mu Chipangano Chatsopano, okhulupirira apasidwa maitanidwe ofanana ndi a Chipangano Chakale. Akuyenera kukhala ansembe kapena otumikira Uthenga Wabwino

**Koma inu ndinu mbadwa yosankhika, ansembe acifumu, mtundu woyera mtima, anthu a mw ni wace, kotero kuti mukalakire zoposazo za iye amene anakuitanani muturuke mumdima, mulowe kuunika kwace kodabwitsa. (1 Petro 2:9)**

Okhulupirira ayitanidwa kuti akachitire umboni wa Mulungu amene wawachosa mu mdima wauzimu kuwapitisa mu kuwala kwa Yesu khristu (Yohane 9:5). Okhulupirira anaudzidwa kuti “ayende koyenera maitanidwe amene munaitanidwa nao” (Aefeso 4:1). Pali mayitanidwe amodzi okha omwe ali kuchitira umboni wa Uthenga Wabwino. Ndi maitanidwe a okhulupirira onse.

Mayitanidwe oti munthu akhale otumikira Uthenga Wabwino satengera maphunziro kapena kutheraka kwawo. Mulungu amagwirisa ntchito anthu osayenera kuti iye mwini alandire Ulemu.

**Pakuti penyani maitanidwe anu, abale, kuti saitaniidwa ambiri anzeru, monga mwa thupi; ambiri amphamvu, mfulu zambiri, iai;**

**Koma Mulungu anasankhula zopusa za dziko lapansi, kuti akacititse manyazi anzeru; ndipo zofoka za dziko lapansi Mulungu anazisankhula, kuti akacititse manyazi zamphamvu;**

**Ndipo zopanda pace za dziko lapansi, ndi zonyozeka, anazisankhula Mulungu, ndi zinthu zoti kulibe; kuti akathere zinthu zoti ziriko;**

**Kuti thupi liri lonse lisadzitamande pamaso pa Mulungu. (1 Akorinto 1:26-29)**

## **MPHATSO YA UVANGELI**

Atumiki ena a Uthenga Wabwino amapatsidwa mphatso zapaderadera kuchokera kwa Mulungu kuti akhale avangeli. Mphatso ya uvangeli ndi kuthekera kufalisa Uthenga Wabwino kwa osakhulupira mu njira yoti amuna ndi akadzi amanvesera nakhala anthu ofunikira mu Thupi la Kristu. Mau oti uvangeli agwiritsidwa katatu mu Chipangano Chatsopano. Pa Aefeso 4:11-12, Paulo adati Mulungu anapatsa amuna ndi akadzi omwe ali ndi mphatso ya uvangeli ku mpingo.

Palibe yemwe angangoganiza kukhala m’vangeli chifukwa amalankhula bwino, ali ndi makhalidwe abwino kapena amakhala bwino ndi anthu osiyanasiyana. Mulungu amayitana

anthu nawakonzekereso kuti akhale avangeli. Pakuyenera kuti pasakhale mpikisano pakati pa azibusa, aphunzisi, komanso avangeli. Uvangeli ndi mbali imodzi ya Mpingo, osati oyima paokha.

Mphatso ya uvangeli ndi imodzi mwa mphatso youlamulo yomwe yaperekedwa ku Mpingo, yomwe cholinga chake ndi kukonzekereso ena pa ntchito yautumiki. Izi zikutanthauza kuti mvangeli sali ndi kuthekera kofalitsa uthenga kwa ochimwa okha basi, komanso kukonzekereso oyera ntima ku uvangeli.

Ingakhale Mulungu amapereka kwa ena mphatso zapaderadera zauvageli, onse okhulupirira akuyenera kugwira ntchito ya uvangeli ndi kufalitsa Uthenga Wabwino kwa ena. Timoteo analimbikitsidwa kugwira ntchito ya uvangeli pa 1 Timoteo 4:5. Utha kukhala kuti mulibe mphatso yapaderadera ya uvangeli koma muli ndi udindo wogwsira ntchito ya uvangeli.

## **ZOTENGERA ZA DOTHI**

**Koma tiri naco cuma ici m'zotengera zadothi, kuti ukulu woposa wamphamvu ukhale wa Mulungu, wosacokera kwa ife; (2 Akorinto 4:7)**

Chuma chimene Paulo amalankhula mu ndimeyi ndicho Uthenga Wabwino. Ingakhale ndinu chotengera cha dothi, thupi lanu ndi Kachisi wa Mulungu. Mutha kukhala kuti simukuziwidwa ndi munthu. Mutha kukhala kuti simukuziwidwa ku dera lanu, mpingo wanu, kapena komwe mumasonkhana. Mutha kukhala munthu wa wamba ndi wogwsira ntchito zawamba. Koma Mulungu atha kukugwirisani ntchito mu uvangeli.

Werengani nkhani ya kuchilitsidwa kwa munthu wopuwala pa Machitidwe 4. Pomwe Peturo ndi Yohane anakaonekera pakati paakulu akulu a M'kachisi, zinali zodziwikiratu kuti anali osaphunzira, opulukira:

**Koma pakuona kulimbika mtima kwa Petro ndi Yohane, ndipo pozindikira kuti ndiwo anthu osaphunzira ndi opulukira, anazizwa ndipo anawazindikira, kuti adakhala pamodzi ndi Yesu.**

**Ndipotu pakuona munthu wociritsidwayoalikuimirira pamodzi nao, analibe kanthu kakunena kotsutsa. (Macitidwe 4:13-14)**

Anthu opulukirawawa anali atalandira moyo watsopano kudzera mwa Yesu Kristu. Moyo omwe unali mwa iwo unapangitsa kuti akhale ndi uvangeli wa mphamvu ndi osintha miyoyo.

Yesu anawakhulupirira atumiki ndi udindo wofalitsa Uthenga Wabwino. anatenga atsodzi kuchoka ku ngalawa zawo ndikuwapanga kukhala atsodzi a anthu. Anakhulupirira kuti anthu a wamba atha kukhala anthu ofunikira kwambiri akapatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera.

Gedion anali mlimi. Paulo anali opanga ma hema. Mose anali oweta zifuyo. Luka anali dokotala pomwe Yosefe anali wandale wankulu. Mulungu atha kukugwirisani ntchito pakusatengera maphunziro anu kapena izo zomwe mumachita.

Pomwe muli ndi chomwe muli sizipindula konse. Ndi zomwe mukupanga pamalo mwe Mulungu wakuikidzani. Pfungulo la uvangeli opindula ndikukhala mamuna kapena nkadza wa Mulungu, pa malo a Mulungu, pochita ntchito ya Mulungu, mu njira ya Mulungu.

## MAFUTSO OZIYETSA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera.

---

---

2. Lembani mwachidule gawo la Mau a Mulungu pa Uvangeli

---

---

3. Fotokozani udindo wa Mulungu pa uvangeli.

---

---

4. Zindikirani gawo la Yesu pa uvangeli.

---

---

5. Lembani mwachidule gawo la Mzimu Woyera pa uvangeli.

---

---

6. Fotokozani gawo la pemphero pa uvangeli.

---

---

7. Zindikirani gawo lanu mu uvangeli.

---

---

8. Tanthauzirani mau oti “umboni”

---

---

9. Tanthauzirani mau oti “atumiki.”

---

---

10. Tanthauzirani mau oti “m’busa.”

---

---

11. Fotokozerani chomwe chikutanthauza pakuyitanidwa kwa atumiki.

---

---

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

## ZOONJERZRA POPHUNZIRA

1. Filipino anali ndi mphatso yokhala m'vangeli (mlaliki). Akutchulidwa kuti mlaliki pa Machitidwe 21:8. Chizolowezi chake cha m'phatsoyi chinaonekara kuyambila pachiyambi pomwe anakumana ndi Khristu. Atakumana ndi Yesu, chinthu choyamba anachichita ndikugawana uthenga ndi Natanayeli (Yohane 1:45-46). Pakutha kwa nthawi, Filipino anatsogolera a Herene anjala kwa Yesu (Yohane 12:21-22). Filipino anadzozedwa ndi munthu ngati ntumiki (Machitidwe 16:1-6), koma anayitanidwa ndi Mulungu ngati mlaliki mu mpingo (Aefeso 4:11-12). Werengani utumiki wa Filipino kuti muonjezere chidziwitso chanu cha mphatso yapaderadera yakukhala mlaliki. Muwerenge za:
  - Uthenga wake: Machitidwe 8:12,35
  - Kaonetseredwe ka mphamvu mu moyo wake: Machitidwe 8:5-8
  - Gawo la ubatizo mu utumiki: Machitidwe 8:12, 36-38
  - Moyo waku nyumba kwake: Machitidwe 21:8-9
  - Mayendedwe ake: Machitidwe 8:4-5,26,40
  - Luso lake lokopa magulu a anthu: Machitidwe 8:6
  - Utumiki wake wa munthu payekhapayekha: Machitidwe: 8:27-38
  - Tcheru lake pa kutsogozedwa ndi Mulungu: Machitidwe 8:26,39
  - Chidziwitso chake cha Mau a Mulungu: Machitidwe 8:3-35
  - mayankhidwe a anthu ku utumiki wake: Machitidwe 8:5,6,8,12,35-39
2. Makhalidwe otsatirawa ndi ofunika kuti mukhale opindula pa utumiki wa uvangeli:
  - (1) Mukuyenera kukhala otsimikizirika pa za chipulumutso chanu
  - (2) Mukhale odzazidwa ndi Mzimu woyera
  - (3) Makhalidwe anu atsamatsiyane ndi umboni wanu wanu wa mau.
  - (4) Mukuyenera kukhala ndi chidziwitso chogwira ntchito cha Mau a Mulungu.
  - (5) Mukuyenera kukhala munthu wa pemphero.
  - (6) Mukuyenera kukhala okhudzika ndi otayika, kudzindikira kuti anthu onse tsogolo lawo ndi Gehena.
3. Poti Mau a Mulungu ndi ofunikira pa uvangeli, mukuyenera kuphunzira mavesi omwe amatsogolera anthu ku chipulumutso. Onani chikonzero chomwe chingakuthanidzeni kupanga izi:
  - (1) Lembani vesi lomwe mukuyenera kuliroweza pa mbali limodzi lapa

## CHAPUTALA 5

### KUPEREKA UTHENGA WABWINO

#### ZOLINGA

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba vesi yotsogolera.
- Kuzindikira mfundo zisanu ndi chimodzi za kaperekedwe ka Uthenga Wabwino.
- Kuzindikira malembo omwe amaonetsa njira yakaperekewe ka Uthenga Wabwino kwa anthu a zikhalidwe zina

#### VESI YOTSOGOLERA:

**kuti ciyanjano ca cikhulupiriro cako cikakhale camphamvu podziwa cabwino ciri conse ciri mwa inu, ca kwa Kristu. (Filemoni 1:6)**

#### CHIYAMBI

Mu Mutu Wachitatu mwaphunzira za chidzalo cha uthenga wa uvangeli ndipo mu Mutu Wachinayi mwaphunzira za otumikira Uthenga Wabwino. Phunziro iri likukamba za aperekedwe kwa uthenga wa uvangeli.

Kaperekedwe ka uthenga ka bwino ndi kufalitsa uthenga kuchokera kwa munthu kupita kwa munthu wina mu njira yoti umalandiridwa osapotozedwa. Cholinga chenecheni cha uvangeli ndi chakuti Uthenga Wabwino ugawidwe mu njira yoti umvetsetseke ndikulandilidwa.

#### KULALIKIRA

Izi ndi mfundo zisanu ndi chimodzi zofunikira pomwe tikupereka Uthenga Wabwino. Ulaliki ukuyenera:

#### KUKHALA NDI ZINTHU ZA KUTHUPI NDI ZA UMULUNGU:

Kupereka Uthenga Wabwino (kulalikira) ndikosiyana ndi mitundu ya kaperekedwe ka uthenga kena ndi kena chifukwa Mau a Mulungu, Mulungu Tate, Mwana, ndi Mzimu Woyera amatengapo mbari. Kugawa Uthenga Wabwino sikungoyankhula kapena kucheza ndi anthu ena. Ndi kulankhulana kwa umulungu komwe kumathandizidwa ndi chuma uzimu cha mphamvu chomwe chimagwira ntchito yotsimikizira ndi kukopa olandira uthenga.

#### KUPITA KWA MAGULU ONSE A ANTHU:

Uthenga Wabwino ukuyenera uperekedwe ku magulu onse a anthu: olemera ndi otsauka, ophunzira ndi osaphunzira, wotukuka ndi wosatutuka. Paulo anatsimukiza izi pommwe anatani:

**Ine ndiri wamangawa wa Ahelene ndi wa akunja, wa anzeru ndi wa opusa. (Aroma 1:14)**

Pomwe anati ali wamangawa amatanthauza kuti chifukwa kwalandira Uthenga Wabwino ali ndi ngongole ndi anthu ena kuti akaugawawe kwa iwo. Anamva udindo uwu kwa anthu onse. Panaline kusiyana kwa magulu a anthu mu malingaliro a Paulo. Alayense amafunikira Uthenga Wabwino. Panalibe yemwe anali otsaukitsita kapena olemeretsa, wachipembedzo kapena wachikunja. Simukuyenera kukhawa a tsankho pogawa Uthenga Wabwino. Ngati mukondera, ndiye kuti mukuchimwa (Yakobo 2:1-4).

## **MUKUYENERA KUKHALA OSAKONDERA PAKATI PA MAGULU NDI MUNTHU MODZI MODZI:**

Chizolowezi cha okhulupirira ambiri ndi kusangalatsidwa ndi khamu la nathu. Azibusa amathera nthawi yawo yambiri kuserii kwa guwa kutsogolo kwa gulu. Pomwe munthu amkhala watayika mu gulu. Izi ndizoona makamaka mu chikhalidwe chomwe kufalitsa uthenga kumatheka kudzera pa kanema ndi wailesi.

Palibe njira yomwe imalowa mmalo mwa utumiki wokumana ndi anthu. Paulo nthawi zambiri amatumikira m'tsonkhano koma fanizo lake laku Atesalonika linali ngat mkazi kusamala mwana ndi atate ndi ana ake (1 Atesalonika 2:7,11). Sanaonetse kukondera pakati pa munthu mmodzi mmodzi ndi kutumikira pa mtsonkhano.

Yesu anatumikira ku khwimbi la anthu, koma anagawanso Uthenga Wabwino ka munthu mmodzi mmodzi ngati mkazi wa ku Samalira, Nikodemo, Zakeyasi, ndi ena otero.

## **UTHENGA UFIKIRE ZIKHALIDWE ZONSE ZA ANTHU**

Zikhalidwe zosiyana ziri di njira zosiyana zopangira zinthu. Izi zinali zoonza ingakhale nthawi ya Baibulo. Mwa chitsanzo, Listira inali dera lachikunja. Atene unali mzinda wotukuka kwambiri ndipo unali ovuta kufikiridwa ndi Uthenga Wabwino. Bereya unalandira Mau a Mulungu ndichimwemwe. Unali kutsaka choonadi.

Kusiyana kwa zikhalidwe, zilankhulo, maphunziro, ndi mitundu kumabweretsa ziphinjo koma zitha kuthetsedwa ndi Uthenga Wabwino kufotokozeredwa mu njira yoti nkulandiridwa. Kumvetsetse chikhalidwe china kumafunikira kukhala ofuna kusintha kaganizidwe ndi kachitidwe ka zinthu. Koma, simukuyenera kusintha kaganizidwe ndi kachitidwe ka zinthu komwe kamaonetsedwa ndi Mawu olembedwa a Mulungu, mutha kusintha mu njira zina zomwe zingathandize kuti mupereke bwino Uthenag Wabwino.

Uthenga Wabwino ukuyenera kuperekedwa mu njira yoti umvetsetseke ndi anthu omwe akumvera. Kalankhulidwe, chilankhulo, ndi njira yoperekera zikuyenera zisinthidwe ndicholinga choti Uthenga Wabwino umvetsetseke. Paulo anadzindikira ndi kuchita ichi (Machitidwe 21:37-40; 22:2).

Machitidwe 26:18 akupereka njira yabwino yoperekera Uthenga Wabwino kwa anthu a zikhalidwe zina. Mulungu anatumidza Paulo kwa Amitundu...

**...kukawatsegulira maso ao, kuti atembenuke kucokera kumdimba, kulinga kukuunika, ndi kucokera ulamuliro wa Satana kulinga kwa Mulungu, kuti alandire iwo cikhululukiro ca macimo, ndi colowa mwa iwo akuyeretsewa ndi cikhulupiriro ca mwa Ine. (Macitidwe 26:18)**

Uthenga Wabwino uperekedwe mu njira yoti:

1. Ukatsegule maso a anthu.
2. Kuti atembenuke kuchokera kumdimba kwa uzimu kupita kuunika.
3. Kuti achokere ku ulamuliro wa Satana kulinga kwa Mulungu.
4. Kuti alandire chikhululukiro cha machimo kudzera muchipulumutso
5. Kuti alandire cholowa cha uzimu kudzera mu kuyeretsewa ndi chikhulupiriro.

Chikhalidwe chimene munthu wakuliramo chimaonetsera zigawo zisanu:

**-Chilankhulo chake:** Mmene amaperekera ndi kulandira uthenga ndi maganizo.

**-Mmene amalionera dziko:** Mnen amalionera ndi kumvetsa dziko.

**-Zikhulupiriro zake:** Chipembezo, zikhulupiriro mu zinthu zauzimu, maganizidwe.

**-Umunthu ake:** Kufunikira, Kuyenera, kapena ubwino omwe amapereka ku zinthu.

**-Makhalidwe ake:** Mmene amachitira zinthu ndi chikhalidwe; zikhalidwe zomvomerezeka ndi mtundu wa anthu.

Muona kuti tchati chotsatirachi Machitidwed 26:18 akukamba zonsezi:

Chilankhulo: Uthenga umaperekedwa bwino, kumvetsetseka, ndi kulandiridwa	
Kutsegula maso awo } kakkuperekedwa	Kaonedwa ka Dziko: Kaonedwe ka Baibulo
Zikhulupiriro:	Uthenga wa chikhulupiriro; Uthenga Wabwino wa Ufumu umasinthia zikhulupiriro zawo.
Kuti atembenukire ndi kulandira }	Umunthu kusintha. Makhalidwe kusintha.

## **PITIRIRANI UTHEKA WAPAKWAMA**

Mawu ndi ofunikira pa kulankhulana. Pakudzera mu Mawu olembedwa, Mulungu amaonetsera chifuniro chake pa anthu. Koma ngati mukufuna kutsata chitsanzo cha atsogoleri a Chipangano Chatsopano, mukuyenera kupitirira uthenga wapakamwa, makamaka mu zikhalidwe zomwe zimakhazikika kwambiri pa zinthu zomwe anthu akumana nazo. Ndi cholinga cha Mulungu kuti anthu akumane ndi choonadi cha Uthenga Wabwino, osati kungomva kokha. Ndichifukwa chake Yesu anati “Pomwe mukupita chilitsani odwala ndi kutulutsa ziwanda.” Kupereka Uthenga Wabwino kumapitirira uthenga wapakamwa. Ndi kuonetsera kwa mphamvu.

## **MUKHALE MOGWIRIZANA NDI MOYO WANU**

Paulo anamuza Filimoni kuti...

**kuti ciyanjano ca cikhulupiriro cako cikakhale camphamvu podziwa cabwino ciri conse ciri mwa inu, ca kwa Kristu. (Filemoni 1:6)**

Paulo amamulimbikitsa Filimoni kuti chikhulupiriro chake chiperekedwe ndi makhalidwe achi Khristu omwe amaonetsera Yesu kwa anthu ena. Palibe kuchuluka kwa mawu kulikonse komwe kungapose mphamvu ya chinyengo, kapena mawu paokha kukwaniritsa zomwe mphamvu ya chitanzo chabwino chingapindure. Kaperekedwe ka Uthenga Wabwino kakuyenera kugwirizana ndi makhalidwe a moyo wanu kuti ukakhale opindula.



## MAYESO OZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera

---

---

2. Lembani mfundo zisanu ndi chimodzi zakaperekedwe ka Uthenga Wabwino.

---

---

---

---

3. Ndi mavesi anji omwe amaonetsa njira ya kaperekedwe ka Uthenga Wabwino kwa anthu omwe ndi a zikhalidwe zina?

---

---

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

## ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Mbali ya kukhala kulumikidzana kwabwino ndikukhala omvetsera wabwino. Nazi mfundo za kumvetsera:
  - Muzipereke nokha kwa thunthu ku ntchito yomvetsera zimene munthu winayo akunena. Kumvetsera siku kusokoneza. Kumatanthauza kuti kugwira chikhumbokhumbo chanu chofuna kulankhula.
  - Kuyika patsogolo zomwe iye akunena. Mutha kuganiza kuti muli ndi yankho, dikirani pokhapkha muli otsimikizika kuti funso ndi chani.
  - Mutsimikizike kuti mwamvetsetsa chomwe olankhula akutanthauza. Apo ayi, funsani funso.
  - Mafunso ndiofunika pakumvetsera. Amathanthinza kufotokoza bwino pa zomwe zikulankhulidwa.
  - Mudzindikire kalankhulidwe kosatulusa mawu. Mukuyenera kukhala atcheru ndi mmene nkhope yake ikupanga, osati mawu okha. Munthu atha kumakambba zina koma nkhope yake kumakambanso zina.
2. Ulaliki wa Paulo umasiyana kutengera mafuko ndi mayiko. Mufananize ulaliki wake mu sinagoge ku Antiokeya pa Machitidwe 13 ndi ulaliki wake ku Atene pa Machitidwe 17.
3. Yesu anali oziwa kulankhula:
  - Anali ndi chidziwitso cha zinthu zam'mbuyo ndi Baibulo: Mateyu 12:38-42
  - Amagwiritsa ntchito zinthu ndi zithunzi zomwe zinali zoziwika kwa anthu: Luka 12:29-32; Marko 4:21-34
  - Anali osavuta, amalankhula za kuwala, mkate, m'busa wabwino, ndi munda wa mpesa: Yohane 6:35; 8:12; 15:1
  - Si nthawi zonse zomwe amapereka yankho, kuma amapereka ziphunziso zake zambiri mu mafanizo ndi mafunso.
  - Amagwiritsa ntchito nthabwala. Mwachitsanzo, kuyerekedza chiduswa mu m'maso mwa m'bale wanu ndi chipika mu maso anu: Mateyu 12:1-23
  - Amagwiritsa ntchito zifukwa: Mateyu 12:1-32

## CHAPUTALA 6

### OLANDIRA UTHENGA

#### ZOLINGA:

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba vesi yotsogolera.
- Kufotokoza ndondomeko ya Mulungu ya kachulukitsidwe ka okhulupirira.
- Kutchula anthu awiri a Muchipangano Chatsopano omwe agwiritsidwa nthito ngati zitsanzo.
- Kuzindikira zinthu zofunikira za uvangeli.
- Kuzindikira mitundu inayi ya anthu ochimwa omwe akambidwa mu Baibulo.
- Muyambe kutumikira.

#### VESI YOTSOGOLERA:

**Ndipo zimene wazimva kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezi uikize kwa anthu okhulupirika, amene adzadziwa kuphunzitsa enanso. (2 Timoteo 2:2)**

#### CHIYAMBI

Mukuphunzira ndongosolo la Mulungu yofikira dziko lonse ndi Uthenga Wabwino

- Yesu ndi chidzalo cha uthenga.
- Ophunzira ndi azitumiki a Uthenga Wabwino apatsdwa mphamvu ndi Mzimu Woyera
- Dziko lonse lapansi ndiro lolandira uthenga.

Masiku ano tikukhala mu dziko lomwe likukula. Zikwizikwi za anthu akubadwa tsiku ndi tsiku. Chiwerengero cha anthu pa dziko chichuluka mofulumira. Pali anthu ochuluka omwe sananve Uthenga Wabwino.

Yesu akufunitsisa kuti okhulupirira afikire dziko lonse ndi Uthenga Wabwino. Mu magawo awiri apitawo mwaphunzira za uthenga komanso za atumiki a uvangeli. Koma ndi khwimbi la anthu lomwe likudikirira uthenga, kodi iwo amene anyamula uthengawo ayambire pati? Kodi chofumikira kwambiri ndi chani ndipo muyambire pati? Kodi yemwe akuyenera kukhala olandira uthenga ndi ndani?

#### KACHITIDWE KOCHULUTSA

Mu Baibulo, Mulungu anabvumbulutsa ndondomeko lapaderadera lothandidza okhulupirira kuti akakwaniritse nthito ya uvangeli. Zakhazikika pa kachuluitsidwe ka uzimu. kachulukitsidwe ndi mfundo zokhuzana ndi kakulidwe ka dziko lapansi. Kukula sikumachitipa pakuyika chinthu chimodzi pa chinzake.

Dongosolo la Mulungu la uvangeli linakhazikika pa mfundo zakachulukitsidwe m'monga m'mene dziko lapansi limachulukitsidwira.

**Ndipo zimene wazimva kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezi uikize kwa anthu okhulupirika, amene adzadziwa kuphunzitsa enanso. (2 Timoteo 2:2)**

Paulo anamuudza Timoteyo kuti asankhe anthu okhulupirika and apereke kwa iwo zinthu zimene anaphunzira. Anthu okhulupirikawa amayenera kukhala ndikuthekera kophunzisa

ena. Pakuzera mudongosolo yakachulukitsidweyi, Uthenga Wabwino ufalikirira pa dziko lonse lapansi.

Kuti muone m'mene ndondomekoyi imayendera, werengani tchati yomwe iri m'musiyi. Tchati iyi ikugwiritsa ntchito nyengo ya pachaka ngati nthawi yapakati yofunikira kutembenuza munthu ku Uthenga Wabwino ndikumuhunzisa kuti akhale Khristu obala zipatso. Koma mu zenizeni, zitha kutenga nthawi yochuluka kapena yochepera, malinagani ndi m'mene munthuyo watengeraop gawo, ndiye ndizosatheka kuyika nthawi yokhazikika. Koma ngati okhulupirira angafikire munthu modzi yekha ndikuwaphunzisa pa chaka chimodzi ndi kuwapangitsa kuti nawo alonjeze kuti aphunzisa munthu modzi pa chaka, dziko lapansi litha kufikiridwa mosavuta ndi Uthenga Wabwino.

Onetsetsani pa tchati kuti mu chaka choyamba okhulupirira akuphunzisa munthu modzi. Pakutha pa chakako, pali anthu awiri okhulupirika, okhulupirira ndi otembenuka watsopano yemwe wamuphunzisa mfundo zofunikira za chikhulupiriro cha chiKhristu.

Mu chaka chotsatiracho, aliyense akufikira munthu modzi ndi Uthenga Wabwino ndi kuwaphunzisa. Pakutha pa zaka ziwiri, pali anthu okwanira anayi, omwe wina aliyense wa iwo aphunzisa munthu modzi modzi mu chaka chotsatiracho.


	OPHUNZISA	OPHUNZIRA	ONSE PAMODZI
CHAKA CHA 17	65,536	65,536	= 131,072
CHAKA CHA 16	32,768	32,768	= 65,536
CHAKA CHA 15	16,384	16,384	= 32,768
CHAKA CHA 14	8,192	8,192	= 16,384
CHAKA CHA 13	4,096	4,096	= 8,192
CHAKA CHA 12	2,048	2,048	= 4,096
CHAKA CHA 11	1,024	1,024	= 2,048
CHAKA CHA 10	512	512	= 1,024
CHAKA CHA 9	256	256	= 512
CHAKA CHA 8	128	128	= 256
CHAKA CHA 7	64	64	= 128
CHAKA CHA 6	32	32	= 64
CHAKA CHA 5	16	16	= 32
CHAKA CHA 4	8	8	= 16
CHAKA CHA 3	4	4	= 8
CHAKA CHA 2	2	2	= 4
CHAKA CHA 1	1	1	= 2

### UVANGELI WOCHULUKITSA

Zindikirani, mutenge mpingo omwe ulu ndi mamembala pafupifupi 100. Muonjezere tchatiyi mpaka anthu 100 aliyense kufikira munthu modzi ndi Uthenga Wabwino ndikuwaphunzisa kuti akhale obala zipatso ndipo mutha kuona m'mene zilili zosavuta kufikira dziko lonse ndi Uthenga Wabwino. Mukaphunzisa modzi kuti akafikire modzi kuti naye akafikire munthu modzi, ophunzira amachuluka mofulumira ndipo kuchulukitsa kumafulumira kusiyana ndi kuphatikiza.


### NDONDOMEKO MU MPINGO WOYAMBA

Chithunzi chotsatirachi chikuonetsa masiteji oyambirira a uvangeli wochulukitsa wochitaka ndi Andreyana, m'modzi mwa ophunzira oyamba a Yesu:



1. Andreya anagawana Uthenga Wabwino ndi m'bale wake, Petulo
2. Petulo anagawa Uthenga Wabwino patsiku la pentekosto ku Yerusalemu,
3. Petulo anapitiliza kugawana ndi anthu ena omwe nawonso anayamba kugawa Uthenga Wabwino.
4. Zikwi zikwi za okhulupirira omwe anafalikira kuchokera ku Yerusalemu anapitiriza kufalitsa Uthenga Wabwino.
5. Munthu wina aliyense anakumana naye amakhala obala zipatso ndipo ndondomekoyi imapitirira.

Chithunzi chomwe chiri munsimu chikuonetsa masiteji oyambira a uvangeli ochitidwa ndi Mntumwi Paulo:



1. Ananiya akugwiritsidwa ntvhito ndi Mulungu pa kuukitsa Paulo.
2. Paulo akuphunzisa Timoteo.
3. Paulo akupitiriza kuphunzisa anthu ena.
4. Timoteo akuphunzisa anthu okhulupirika omwe angakaphunzise anthu ena.
5. Anthu okhulupirira akufikira anthu ena.
6. “anthu enawa” akupitiriza ndondomeko ya kkachulukitsidwe.
7. Munthu wina aliyense akupitiriza kuchulukitsa.


### ZINTHU ZOFUNIKIRA PA UVANGELI

Mau a Mulungu amaonetsera zinthu zofunikira pa uvaneli zingapo. Zinthuzi ndi:

#### MAUBWENZI OPEZEKERATU:

Chipangano Chatsopano chimationetsera kuti Uthenga Wabwino unafalikira bwino pamene panali ma ubwenzi opezekeratu. Mwa ichi tikutanthauza kuti mutha kufalitsa Utthenga Wabwino mosavuta kwa abwenzi omwe muli nawo, achibale ndi ogwira nawo ntchito.

Mwa chitsanzo, Yesu anyitana msodzi m'modzi otchedwa Andreyha. Andreyha anagawana Uthenaga Wabwino ndi m'bale wake otchedwa Petulo. Anagawa uthengawu kwa asodzi omwe amagwira nawo ntchito. Posatenga nthawi gulu la asodzi linayamba kutsatira Yesu.



Tsopano onani pa chithunzipo. Onetsetsani pa mivi yomwe ikuchokera kwa abwenzi anu kupita kwa INU. Inu ndinu Kazembe wa Ambuye kwa anthu awa. Atha osalowa mu kachisi. Athanso osalumukizana ni m'busa wa mpingo wanu. Koma INU mukuwaziwa bwino. Ndikudzera mwa ubale omwe ulipo kale umene mungayambire kuwalalikira.

## **MABANJA**

Banja linakengedwa ndi Mulungu ngati

Mose anali okhulupirika ndi apabanja ake onse, anafuula kuti “koma ine, ndi a m'nyumba yanga, tidzatumikira Yehova” (Yoswa 24:15). Rahabu, mkazi wadama waku Yeriko, anatembenukira kwa Ambuye ndi kupulumutsa banja lake lonse ku chionongeko (Yoswa 2). Pamene Yesu anayendera banja la Zakaliya, analengeza kuti, “Lero cipulumutso cagwera nyumba iyi” (Luka 19:9). Pamene yesu anachilitsa mwana wa mkulu wa mfumu, iye anakhulupirira pamodzi ndi apabanja lake lonse (Yohane 4:46-54).

Banja lonse la Komeliyo linabwera kwa Ambuye (Machitidwe 10), mongaso momwe linachitira banja la Lidiya (Machitidwe 16) ndi mdindo waku Filipo (Machitidwe 16), Krispo (Machitidwe 18:8), ndi Stefana (1 Akorinto 1:16).

Pamene Yesu anati pazakhala kugawanikana pakati pa mabanja chifukwa cha Uthanga Wabwino, izi nthawi zina zimachitika chifukwa njira za uvangeli osati chifukwa cha Uthanga Wabwino. Uvangeli ukachitika pakati pa banja, mphamvu ya Mulungu ya machilitso ndi kubwezeretsa itha kuyenda pakati pa banjalo.

Mamembala a banja akafikiridwa ndi Uthenga Wabwino kunja kwa banja, amakopedwa kuchoka ku paubale wapabanja natsiyantsidwa ndi anthu omwe akuyenera kukhala nawo limodzi. Banja lomwe limaopa kulowerera, litha kukhala m'dani wa otembenuka ntima, ndikukana Uthenga Wabwino. Uvangeli wa banja lonse umapereka ulemu kwa gulu la anthu lomwe Mulungu analenga. Banja limapereka mphamvu kwa otembenuka watsopano osati otsutsana naye.

## **ANTHU OMWE SANAFIKIRIDWE**

Anthu omwe sanafikiridwe ndi Uthenga Wabwino ndiofunikanso kwambiri. Pali mitundu ya anthu ochuluka omwe sanafikiridwe ndi Uthenga Wabwino. Anthu ena ambiri sanapeze

kuthekera kowerenga uthenga wa Mulungu kwa iwo omwe unalembedwa M' mau a Mulungu chifukwa uthengawu sunatanthaudziridwe mudzilankhulo zawo.

Tikamaona Dziko lapansi monga ngati mayiko, titha kunena kuti dziko lonse lafikiridwa chifukwa dziko lonse kuli anthu omwe akuchita umboni wa Uthenga Wabwino. Mu dziko lina liri lonse padziko lino lapansi kuli okhulupirira ndi mipingo yokhazikika. Koma izi sizikufanana ndi “anthu amafuko onse, manenedwe ndi anthu a mitundu yonse” mmonga zalembedwera pa Chibvumbulutso 5:9.

Pamene Yesu analankhula zakupita ku dziko lonse lapansi samatanthauza mayiko okha ayi. Mau omwe Yesu anagwirisa ntchito pamene anakamba za dziko anali mau achi Greek oti “ethne.” Mauwa amatanthauza kuti “fuko” kapena kuti “mitundu ya anthu.” Yesu amaona dziko lapansi ngati “anthu onse” kapena kuti “mitundi ya anthu.”

Mtundu wa anthu umatanthauza kuti:

*“Gulu lalikulu la anthu omwe lomwe lamangiridwa pamodzi. Litha kumangiridwa pamodzi ndi chilankhulo, zikhalidwe, miyambo, ndi malo omwe akukhalako”*

Mtundu wa anthu ndi gulu la anthu omwe lingafikiridwe ndi Uthenga Wabwino mosavuta popanda kukumana ndi mavuto akusamvetsetsana and kulandilidwa. Chifukwa mtundu wa anthu umalankhula chilankhulo chofanana ndiponso amakhala ndi zikhalidwe zofanana, zilankhulo ndi zikhalidwe zosiyana zomwe zimalepheretsa kaperekedwe ka Uthenga Wabwino zimachotsedwa.

Pali zikwizikwi za mitundu yosiyanasiyana ya anthu pa dziko lapansi imene yazindikiridwa kufikira tsiku lalero. Ina ili ndi anthu ochepa pomwe ina ili ndi anthu ochuluka. Chilumba chirichonse cha pa dziko lapansi sichinapangidwe ndi mayiko osiyanasiyana okha, komanso ndi mitundu yosiyanasiyana ya anthu. Mwa chitsanzo, pa chilumba cha Africa pali anthu zikwizikwi za zilankhulo komanso mitundu ya anthu yambiri.

Mtundu omwe wafikiridwa ndi Uthenga Wabwino ndi mtundu omwe uli ndiokhulupirira komanso zipangizo zokwanira kulalikira anthu awo omwe posafuna chithandizo kuchokera kwina.

Mtundu osafikiridwa ndiumene uli ndi anthu komanso zipangizo zosakwanira kuti ungate kulalikira Uthenga Wabwino kwa anthu awo omwe posafuna chithandizo kuchokera kwina. Pali zikwizikwi za mitundu ya anthu yomwe iribe mpingo womwe ungakwanise kuchitira umboni pa iwo wokha. Mkati mwa mitunduyi muli anthu ochuluka kwambiri. Anthu omwe sanafikiridwewa atha kuyikidwa m'magulu akuluakulu, omwe ali, anthu achikhalidwe, Asilamu, Achina, Ahindu, ndi Abuda.

Paulo anaonetsa kuti anthu oyamba kuwalalikira akuyenera kukhala omwe sanafikiridwe:

**Ndipo coteru ndinaciyesa cinthu caulemu kulalikira Uthenga Wabwino, pa malopo Kristu asanachulldwe kale, kuti ndisamange nyumba pa maziko a munthu wina.**

**Koma monga kwalembedwa, Iwo amene uthenga wace sunawafikire, adzaona, Ndipo iwo amene sanamve, adzadziwitsa. (Aroma 15:20-21)**

#### **MALO OLANDIRIDWA:**

Yesu anaphunzisa ophunzira ake kuti asakatunikire ku malo omwe sanalandiridwe. Ngati Uthenga wakanidwa, amayenera kuchokako and nakhazikika ku malo omwe alandiridwa. Paulo naye anatsatira njira iyi.

## **MIZINDA:**

Muphunzira mu phunzirori mmene Paulo ankhazikitsira mipingo mu mizinda otukuka. Kusintha zawi zonse kumayambira m'mizinda kenako kumafalikira ku malo akumidzi. Mizinda ndi malo a zamalonda ndi zokopa alendo ndipo anthu omwe omwe amabwera amafikiridwa ndi Uthenga Wabwino amatenga uthenga pamene akubwerera kwawo.

## **MITUNDU INAYI YA OCHIMWA**

Ingakhale anthu amasiyana mitundu, Baiulo imaonetsera za makhalidwe ena a anthu kulikonse. Anthu onse kupatula Mulungu ndi ochimwa. Yotsatirayi ndi mitundu inayi ya anthu ochimwa yomwe yakambidwa m'Baibulo.

## **WOCHIMWA MWADALADALA:**

Pa Aroma 1:18-32 akufotokodera za wochimwa mwadaladala. Wochimwa mwadaladala amakhulupirira kuti kuli Mulungu koma izi zokha sizingapulmutse munthu. Wochimwa mwadaladala ndi wanzeru, ndipo ukayesera kumubweretsa Uthenga Wabwino iye amabweretsa bvuto laluntha. Ichi ndichifukwa chake mukuyenera Kudziwa Mau a Mulungu. Baibulo limati:

**...okonzeka nthawi zonse kucita codzikanira pa yense wakukufunsani cifukwa ca ciyembekezo ciri mwa inu, komatu ndi cifatsondi mantha. (1 Petro 3:15)**

## **WOCHIMWA WOSINTHIKA:**

Aroma 2:1-16 imafotokodza wochimwa wosinthika. Wochimwa wosinthika amakhulupirira kuti Mulungu aliko chifukwa timaphunzira pa Aroma 2:3 kuti amaganiza ali ndi kuthekera koweruza ochimwa omwe akambidwa pa Aroma 1:18-19. Komanso amakhulupirira kuti azathawa chiweruza cha Mulungu. Wochimwa wosinthika amaganiza kuti ndiwabwino ngati munthu wina aliyense ndikuti mu mpingo muli anthu achinyengo. Ndi m'nthundu wa munthu yemwe amayetsa kusintha mwa iye yekha.

## **WOCHIMWA WACHIPEMBEDZO:**

Aroma 2:17-23 imafotokodza za ochimwa achipembedzo. Ochimwa achipembedzo ndi amene amakhulupirira mu chipembedzo chake ndi mpingo wake pa chipulumutso. Amakhulupirira mu miyambo, koma sadziwa Mulungu modzi woona. Nikodemo anali Nfarisi (Yohane 3:1). Anali wachipembedzo, koma samamvetsetsa tanthauzo lenireni la chipulumutso ndi kubandwanso mwatsopano.

## **OCHIMWA OKANIDWA:**

Mkazi wapachitsimwe pa Yohane 4 ndi chitsanzo cha wochimwa okanidwa. Anali wothamangitsidwa, ukwati wake unatha, ndipo ndizachidziwikire kuti azikadzi adzake amamutsala chifukwa nthawi zambiri akazi amakatunga madzi limodzi. Mkaziyu abwera yekha.

Ochimwa okanidwa amakhuzidwa ndi mavuto ake okha kusiyana ndi zinthu za uzimu. Njira yabwino yomufikira ndi ngati yomwe Yesu anagwiritsa ntchito pofikira mkazi pa chitsime. Mutha kuyamba ndikufikira zosowa za moyo wawo.



## MAYESO OZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera.

---

---

2. Kodi ndondomeko ya Mulungu ya kachulukitsidwe ka okhulupirira ndi yotani?

---

3. Kodi anthu awiri a Muchipangano Chatsopano omwe agwiritsidwa ntchito ngati zitsanzo ndi ati?

---

4. Kodi zinthu zofunikira za uvangeli ndi ziti?

---

5. Kodi mitundu inayi ya anthu ochimwa omwe akambidwa mu Baibulo ndi iti?

---

---

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

## ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Mwapemphero malizitsani lonjezo lotsatirari ndipo muyambe kuzichita:

*“kuzindikira kuti uvangeli ndi udindo wa okhulupirira wina aliyense, Ine ndiripano kuzipereka ndekha kupempherera munthu modzi, kuchita kothequera kugawana naye Uthenga Wabwino, ndikuwabweresa mu chiyanjano ndi Kristu ndi Mpingo.”*

Munthu yemwe ndingamupempherere ndikutumikira ndi:

Kusaina: \_\_\_\_\_

Tsiku: \_\_\_\_\_

2. Pa Luka 16:19-31 pali nkhani ya munthu wachuma yemwe anapita ku Gehena. Munthu uyu amafuna kubwerera kukagawa Uthenga Wabwino kwa apa banja pake koma nthawi inali itatha. Musadikire kuti nthawi ithe kaye kugawa Uthenga Wabwino ndi apa banja panu.
3. Muphunzire zambiri za kachulukitsidwe ka uzimu pakupeza phunziro la Harvestine International Institute, *“njira za kachulukitsidwe.”*
4. Umu ndi m’momwe munga mukukweza ogwira ntchito yokolola:
  - Muzipempherera ogwira ntchito: Mateyu 9:8; Yakobo 4:2; Luka 11:9; Yohane 14:14
  - kulalikira ogwira ntchito: Yesaya 6:8
  - Muzipezekese nokha kwa iwo ndikuwakonzekeresaka monga m’mene Yesu anachitira: Mateyu 20

## CHAPUTALA 7

### NJIRA: MFUNDO ZA CHIPANGANO CHATSOPANO

#### ZOLINGA

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba vesi yotsogolera.
- Lembani mwachidule mfundo zofunikira za uvangeli wa Chipangano Chatsopano.
- Kutotokoza zotsatira za uvangeli wa Chipangano Chatsopano

#### VESI YOTSOGOLERA

**...Omwe aja asanduliza dziko lokhalamo anthu, afika kunonso. (Macitidwe 17:6)**

#### CHIYAMBI

Phunziro iri ndi chiyambi cha maphunziro omwe akukamba za njira za uvangeli. Njira ndi ndondomeko zoyikika bwino zogwirisara ntchito popanga zinthu. Ngati mujufuna kukhala opindula pa uvangeli, mukuyenera kugwirisa ntchito njira za mmalembo. Njira zina zimene zavomeredzedwa ndi anthu omwe achitapo uvangeli ndizololedwa.

Phunziro iri likukamba za njira zomwe zikupezeka m'Chipangano Chatsopano. Phunziro lachisanu ndi chitatu likukamba za njira zomwe zabvumbulutsidwa mu zifanizo zauvangeli zomwe zinalembedwa mu Chipangano Chatsopano. Ndime ya Chisanu ndi Chinayi ikukamba mmene mungapangire uvangeli pa inu nokha ndipo Ndime yachi Khumi ikukamba zaziphinjo zomwe zimapezeka mukamapanga uvangeli.

Pamene mukuyamba kuphunzira njira za uvangeli, mukuyenera kudzikambira kuti pali njira zina zomwe zavomeredzedwa, Mulungu atha kukhala ndi njira ina yomwe iri yosiyana ndi njira zina zonse pofuna kuti inu mukapindure mu uvangeli wanu. Pomwe mukugwira ntchito ya uvangeli, nthawi zonse muzimufunsa Mzimu Woyera kuti akupatseni inu kudzodza kwake. Amadziwa ntima wamunthu yemwe mukumutumikira. Ndi udindo wa Mzimu Woyera kukutsogolerani komanso kukudzodzani inu, kukupatsani kunvetsetsa komanso ntima okhudzidwa ndi anthu ena, komanso kokopa omwe sanapulumsidwe ndikuwapangisa kuti avomweredze Uthenga Wabwino.

#### UVANGELI WACHIPANGANO CHATSOPANO

Mabuku a Uthenga Wabwino, Machitidwe, ndi Makalata amasonyeza njira zosiyanasiyana za uvangeli. Munthawi ya Chipangano Chatsopano uvangeli unali wo”

#### TSIMIKIDZIDWA NDI PEMPHERO

Pemphero ndi imodzi mwa njira m'Malembo za uvangeli. Pomwe Yesu amaona zokolola za m'munda ngati zokolola za uzimu za dziko lotayika mu uchimo, chinthu choyamba kulamula chinali kupemphera. Yesu sanati:

- “Zotuta zichulukadi, pitani.”
- “Zotuta zichulukadi, linganizani.”
- “Zotuta zichulukadi, pangani dongosolo.”
- “Zotuta zichulukadi, pazani chuma cha uvangeli.”
- “Zotuta zichulukadi, phunzisani ena.”

Iye anati: “Zotuta zichulukadi, PEMPHERANI...”

Mu Chipangano Chatsopano timaphunzira kuti mpingo wakale nthawi zonse umakhala ukupemphera (Machitidwe 1:14). Ulendo woyamba wautumiki unabadwa mu pemphero (Machitidwe 13:3). Paulo analimbikitsa kuti mpingo uzimupempherera pomwe iye akulalikira (2 Atesalonika 3:1).

Tikuyenera kusiya kudalila pazimene timaziwa za utumiki, anthu omwe sanafikiridwe, komanso njira zofalitsira Uthenga Wabwino. Izi ndizabwino ndithu, koma tikuyenera kukhazikika kwambiri pa lamulo loyamba: “INU PEMPHERANI.”

### **CHOLINGA CHOYAMBA CHOFUNIKIRA:**

Uvangeli siunali chochita chimodzi mwazochita zochulukira za mpingo woyamba, unali chochita chofunikira kwambiri. Lero, uvangeli ndi kutumikira kumakhala kutali pazinthu zofunikira pa anthu ambiri ngakhale mpingo.

Mu nthawi ya Chipangano Chatsopano, uvangeli umachitika mowirika. Umachitika mowirikidza ndi okhulupirira onse. Nchitidwe wake unali opita komwe kuli anthu ndikukawatumikira. Matsiku ano, timawaitana anthu ku mpingo athu nayembekedzerakuti abwera. Matsiku anu mpingo umayitana, pomwe poyamba paja mpingo umapita komwe kuli anthu.

Ali yense amagwira ntchito yauvangeli (Machitidwe 1:8). Aliyense amatenga kufalitsa uthenga ngati lamulo la pa iye yekha kuti akallalikire. Amachita izi kuli konse, osati mu mpingo wawo okha (Mark 16:20). Amachita izi tsiku ndi tsiku (Machitidwe 5:42). Mpingo uli onse umabara zipatso, okhulupirira aliyense amabala zipatso, ndi banja lina liri lonse linali malo a uvangeli.

Pakafunikira, okhulupirira amagwira ntchito ndicholinga chofuna azizithandiza okha pomwe akufalitsa Uthenga Wabwino. Paulo Ntumwi amapanga izi. Zitha kumaoneka ngati zinthu zopusa pomwe munthu waluso ngati Paulo, wamaphunziro komanso yemwe anali ndi mphatso zamzimu ndikumagwira ntchito ndicholinga chofuna kuthandiza utumiki wake. Anali ndi ufulu wonse wofunsa chithandizo kuchokera ku mpingo (1 Akorinto 9:7-15; 1 Timoteo 5:17-18; Galatians 6:6), koma panthawi yomweyo anali okonzeka, ngati panali kufunikira kuterp, kuzithandiza yekha pofuna kufalitsa Uthenga Wabwino. Anachita izi panthawi zingapo. (1 Akorinto 4:12; 1 Atesalonika 2:9; 2 Atesalonika 3:8).

Masiku ano m'mayiko anambiri mwambo wake ndiwakuti azibusa komanso alaliki amalipiridwa Kamba ka khama lawo. Izi zapangaisa kuti ntchito yofalitsa Uthenga Wabwino komanso kubzala mpingo yatsopano iyime. Okhulupirira amasiya ntchito yan uvangeli ndikukhala azitumiki apampingo ndicholinga choti “adzilandira malipiro.” Palinso mpingo ina yochulukira yomwe lilibe azibusa Kamba koti singakwanise kumusamalira m'busa ndipo kuthekera kogwira ntchito sikunaganiziridwe.

Ngati tikufuna tifikire mayiko onse ndi Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu, tikuyenera kutsogoza uvangeli pachinachilichonse. Tikuyenera kulalikira kulikonse, tsiku lina lirironse, komanso ngati kuli kofunikira, yambani ntchito ndi mudzigwira ntchito ndicholinga chofuna kufalitsa uthenga.

### **KUTSOGOZEDWA NDI MZIMU WOYERA**

Mukachitidwe kalikonse ka uvangeli omwe unalembedwa mu Machitidwe, Mzimu Woyera ndiamene amalimbikitsa ndi kupereka mphanvu. Mumakachitsi amakono, makamaka akuulaya, maluso amasaliridwe, ndi mitsonkhano ya akuluakulu a mpingo yatenga malo a Mzimu.

Mzimu Woyera ndiye otsogolera uvangeli. Pali ndime zambiri mu Machitidwe zomwe zimatsonyeza mwachitsanzo ntchito za Mzimu Woyera, koma zotsatirazi ndi ndimezi kuluzikulu pa uvangeli.

-Machitidwe 1:8: Mzimu Woyera ukupereka mphanvu ku umboni wa okhulupirira

-Machitidwe 2: Mphatso ya Mzimu Woyera inaperekedwa ndi kulonjezedwa kwa ohulupirira onse

-Machitidwe 4: Petulo, odzazidwa ndi Mzimu Woyera, anachitira umbozi za chozizwa chomwe chinachitika ndi munthu wopuwala pa Mchitidwe 3

-Machitidwe 4:31 Onse anadzazidwa ndi Mzimu Woyera ndipo analankhula Mau a Mulungu molimbika ntima.

-Machitidwe 5:52: Peturo analengeza kutindife ochitira umboni ndi Mzimu woyera

-Machitidwe 7:51: Stefano anawalamulira akuluakulu a Ayuda omwe sanalandre Uthenga Wawibwino pakukana Mzimu Woyera.

-Machitidwe 9:17: Pailo anadzazidwa ndi Mzimu Woyera anatembunuka ntima.

-Machitidwe 10: Mzimu Woyera unagwera panyumba ya Cornelius, kuwabweresa onse kukutembunuka ntima.

-Machitidwe 11:12: Peturo anafotokoza kuti anapita ku Ceasarea chifukwa Mzimu Woyera unamulamulira iye kutero

-Machitidwe 13:2: Mzimu Woyera anayitana Paulo ndi Banaba ku ntchito ya uvangeli.

-Machitidwe 16:6: Mzimu Woyera unamuletsa Paulo kulalikira ku Asia.

Mzimu Woyera amatsogolera uvangeli mu Mau onse a Mulungu, kudzera mu malangizi auzimu, pakuitana ndi kuwathanatira ogwira ntchito, ndikutenga ndondomeko zathu ndikuzigwirizanitsa ndi zolinga za Mulungu.

### **KUKWANIRITSA PODZERA MU KUKONZEKERA MWACHINDUNJI:**

Pamene Yesu ananamba utumiki wake, analengeza za chikonzero cha mfundo zisanu ndi chimodzi:

**Mzimu wa Ambuye uli paine, Cifukwa cace iye anandidzoza Ine ndiuze anthu osauka Uthenga Wabwino: Anandituma Ine kulalikira am'nsinga mamasulidwe, Ndi akhungu kuti apenyenso, Kuturutsa ndi ufuru ophwanyika, Kulalikira caka cosankhika ca Ambuye. (Luka 4:18-19)**

Yesu anasatira chikonzero chimenechi mu utumiki wake onse wa dziko lapansi, ndipo mpingo woyamba kunapitiriza chikonzero chimenechi.

Pakupita panthawi Yesu anapereka chikonzero chokunza Uthenga Wabwino ku mayiko onse a dziko lapansi (Machitidwe 1:8). Ophunzira amayenera kulalikira kayemu Yerusalemu, kenako apite ku Yudeya, Samaliya, ndikufikira kumalekezero ake a dziko. Iyi ndi chikonzero cha Ambuye. Mukuyenera kuyambiri komwe muliko ndikupitiriza kuonjezera kufikira mutayamba kumakhuza mayiko a dziko lapansi.

“Yerusalemu” wanu ndi dera lomwe mumakhalamo. Pali Akhristu zikwi zikwi omwe amapereka chuma chawo ndi kupempherera utumiki, koma sanatengepo mbali ndikumuuza n'nasi wawo za Uthenga wa Yesu. Mipingo ina iri ndimatumiki opambana akunja kwa dziko

lawo, koma palibe chomwe akupanga kuti alalikire mu deralwo, kupatulo iwo omwe amabwera mu makachisi mwawo.

### **KUTSUTSIDWA NDI SATANA**

Mtsutso wa satana unagwiridwa ntchito ndi Mulungu mu Chipangano Chatsopano pofuna kufalitsa uvangeli. Werengani ndime zotsatirazi:

- Machitidwe 12:1-24: Herodi anapha Yakobo, kenako anamanga Petulo. Izi zinali mtsutsano wan dale.
- Mchitidwe 16:15-40 ndi 19:23-41: Uvangeli unatsemphana ndi zokhumba za malonda mu m'mizinda ya Aefeso ndi Filipo. Mazunzo anayamba kucholera ku dziko ladhachuma.
- Machitidwe 4-7: Mu ndimi izi muli nkhanu ya mazunzo ochokera ku akuluakulu achipembezo.
- Machitidwe 11: Ndime iyi ikukamba za kutsutsana kochechera mu mpingo iwo mwini chifukwa cha chikhalidwe cha Ayuda. Uyu ndi mtsutso wankati.
- Mchitidwe 8, 13, ndi 16: Ndime izi zikukamba za kutsutsidwa ndi satana kudzera kwa Simoni, Elymas, ndi nsikana wogwidwa ndi ziwanda.

Mukamalanda ufumu wa Satana ndi Uthenga Wabwino, mukuyenera kuyembekezera kutsutsidwa kuchokera kun dale, za chuma, ndi dziko lachipembezo. Komatso mudziyembekedzera kuukira kochokera mu mpingo ndi kuukira kochokera kwa satana. M'malo molola kuti mitsutsoyi ikuyimitseni, muyigwiritse ntchito ngati mwayi opititsa matsogolo Uthenga Wabwino ngati m'mene anachitira mu Chipangano Chatsopano.

### **CHILUNJIKO CHA PA GULU NDI ANTHU:**

Njira zonse za uvangeli wa Chipangano Chatsopano zitha kuonedwa mwa uvangeli wa munthu modzimodzi kapena uvangeli wag ulu. Utumiki wa Yesu, ophunzira, Paulo Ntumwi, ndi ena otero anaonetsera kufunika kwa njira zonse ziwiri.

Yesu anatumikira kwa magulu akuluakulua a anthu pomwe iye anali pano pa dziko. Machitidwe awa amakhadzikika mu malingaliro athu chifukwa cha chisangalalo chomwe chinalipo. Koma kuchokera pachiyambi mpakana kumathero a utumiki wake Yesu mwapadera amalalikira kwa amuna ndi akadzi modzi modzi mwa iye yekha. Mu faniza la nkhuso yosokera pa Luka 15:3-7, Yesu amafotokoza za njira yake ya uvangeli, chifukwa anazitchula iye mwini M'busa Wabwino.

Petulo analalikira kwa khamu la anthu ku Yerusalemu pa pentekoste (Machitidwe 2). Iyi inali uvangeli wag ulu. Kumanso anagawana Uthenga Wabwino ndi koneliyasi (Machitidwe 10). Uwu unali uvangeli wa pa munthu. Filipo analalikira kwa khamu la anthu ku Samaliya (Machitidwe 8:5-6) komanso kwa munthu waku Ethiopia mu chipululu (Machitidwe 8:27-35). Paulo anali ndi khwimbi la anthu mu misonkhano yake ina yomwe imathera muzachiwawa! Koma sanatsiye kuchita ndi munthu modzi modzi.

Musatengeke ntima ndi khwimbi la anthu ndikuyiwara kulalikira kwa munthu modzi modzi. Yesu mowirikiza amayitana modzi modzi kuchoka mu khwimbi ndikuwakanidza iwo ndi Uthenga Wabwino wa Ufumu. Uvangeli onse wotumikira munthu modzimodzi komanso wa gulu ndi njira zomwe zikupezeka mu Baibulo.

### **KUTSAGAZANA NDI CHIONETSERO CHA MPHAMVU:**

Uvangeli wa Chipangano Chatsopano umatsagazana ndi chionetsero cha mpamvu ya Mulungu. Yesu analamulira omphunzira ake, “pomwe mukupita... chiritsani odwala, tulusani ziwanda.”

Chionetsero cha mphamvu ya Mulungu imatenga mau omwe mukulankhula ndikuwapanga kukhalala ochitachita:

**...mau ace anali ndi ulamuliro... Ndipo anthu onse anadabwa, nalankhulana wina ndi mnzace, nanena, Mau amenewa ali otani? cifukwa ndi ulamuliro ndi mphamvu angolamulira mizimu yonyansa, ndipo ingoturuka. (Luka 4:32,36)**

Chionetsero cha mphamvu chimatsimikiza Mau ndi zizindikiro zakutsatapo:

**Ndipo iwowa anaturuka, nalalikiraponseponse, ndipo Ambuye anacita nao pamodzi, natsimikiza mau ndi zizindikilo zakutsatapo, Amen. (Marko 16:20)**

Mphamvu ya Mulungu yochilitsa imakhalapo mukamapanga uvangeli:

**Ndipo panali tsiku limodzi la masiku awo, iye analikuphunzitsa; ndipo analikukhalapo Afarisi ndi aphunzitsi a malamulo, amene anacokera ku midzi yonse ya ku Galileya, ndi Yudeya ndi Yerusalemu: ndipo mphamvu ya Ambuye inali ndi iye yakuwaciritsa. (Luka 5:17)**

Mphamvu ya Mulungu imabweeresa chiombolo:

**Ndipo pamene Iye anadziitanira ophunzira ace khumi ndi awiri, anapatsa iwo mphamvu pa mizimu yoipa, yakuiturutsa, ndi yakuciza nthenda iri yonse ndi zofoka zonse. (Mateyu 10:1)**

Mphamvu ya Mulungu imatsimikiza Uthenga Wbwino. “Kutsimikiza” kumatanthauza kuvomereza chinachake. Mpamvu ya Mzimu Woyera imatsimikiza chenicheni cha Mau a Mulungu.

**Ndipo khamu lalikuru la anthu linamtsata iye, cifukwa anaona zizindikilo zimene anacita pa odwala. (Yohane 6:2)**

Chionetsero cha Mpamvu chimatsogolera anthu kwa Mulungu:

**Ndipo mau anga ndi kulalikira kwanga sanakhala ndi mau okopa a nzeru, koma m'cionetso ca Mzimu ndi ca mphamvu; kuti cikhulupiriro canu cisakhale m'nzeru ya anthu, koma mu mphamvu ya Mulungu. (1 Akorinto 2:4-5)**

Muphunzira zambiri za chionetsero cha Mphanvu ndi uvangeli mu gawo lachiwiri ya phunzirori yotchedwa “Pomwe Mukupita.”

## **MAYENDEDWE ABWINO**

Okhulupirira a mpingo woyamba nthawi zonse anali kuyenda chifukwa cha Uthenga Wabwino, nalowerera m'madera omwe anali okonzeka kulandira Mawu. Izi ndi zomwe timati “mayendedwe abwino” zomwe zikuthanthauza kuti kukhala okonzeka kupita mwachangu kumalo komwe kuli kokonzeka kulandira Uthenga Wabwino.

Pa Machitidwe 8:1, timapeza kuti mpingo unakakamizidwa mu mayendedwe abwino chifukwa cha madzuzo. Pomwe okhulupirira anali kumwazikana chifukwa cha madzuzo ku Yerusalemu, “anapita kulikonse kukalalikira Mau.”

Pa Machitidwe 8 pali chitsanzo chabwino cha mayendedwe abwino. Pomwe Filipino anali ku Samaliya kukolola zokolola zambiri za uzimu, Ambuye anamuyitana kuti apite ku chipululu. Mulungu anali naye ndi ntchito ya munthu waku Aitiopiya amane anatengapo gawo lopambana polalikira Africa. Posakhalisa Filipino anachoka ku Samaliya napita ku chipululu.

Ngati tikufuna kunvetsesa mayendedwe abwino, tikuyenera kukhala ndi malingaliro a “okolola” ndi a “msirikali.” Pa Mateyu 9:36-38, Yesu anayerekeza uvangeli ndi kukolola kwachirengedwe. Ngati tikufuna kututa zokolola, tikuyenera kupita komwe zokololo zacha. Tikuyenera kukhala wofunitsitsa kupita kapena kukhala pofuna kukhala ndi zokolola.

Tikuyeneranso kukhala ndi malingaliro a msirikali. Pamene tinakhala okhulupirira, tinapezeka mu ankhondo auzimu a Ufumu wa Mulungu. Tinaitanidwa kuti “tikapirire mavuto ngati msirikali” (2 Timoteo 2:3). Msirikali samabwerera kapena kupuma chifukwa zinthu zafika povuta. Kuyesedwa kwa msirikali simaonekedwe ake pa perete, koma machitidwe ku malo ankhondo.

Msirikali samasankha ntchito yomwe agwire ndipo samagwira ntchito potengera ndi malamulo omwe napsidwa zaka makumi awiri zapitazo. Anali malamulo abwino nthawi imeneyo, koma popita kwa nthawi latha mphanvu zake. Motero, msirikali wa Yesu Khristu amakhala okonzeka ku ntchito ndi mabvumbulutso zatsopano kuchokera kwa Mzimu Woyera.

Yesu amalankhula za mayendeedwe pamene anawauza otsatira ake kuti sakuyenera kupitiriza kufesa panthaka yosabereka.

**Ndipo yemwe sadzakulandirani inu, kapena kusamva mau anu, pamene mulikuturuka m'nyumbayo, kapena m'mudzimo, sansani pfumbi m'mapazi anu. (Mateyu 10:14)**

Paulo anatsatira lamulo iri la “kusasa pfumbi.” Pa Machitidwe 13:51-52 utumiki wa Uthenga Wabwino unakanidwa ku Antiiokeya wa Pisidiya, choncho Paulo anachokako napita ku Ikoniyo. Yesu anali woyendayenda. Amayenda mudzi ndi mudzi kugawa Uthenga Wabwio. Pomwe ophunzira anayesera kuti azitumikira mu dera limodzi, Iye anati:

**Koma anati kwa iwo, Kundienera Ine ndilalikire Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu ku midzi yinanso: cifukwa ndinatamidwa kudzatero. (Luka 4:43)**

### **KUKWANIRITSA KUDZERA POLUMIKIZANA NDI ANTHU ENA:**

Kulumikizana ndi anthu ena ndi njira imodzi ya uvangeli yopezeka mu Chipangano Chatsopano. Kulumikizana ndi anthu ena kukutanthauza kugwira ntchito pamodzi ngati gulu, anthu kugwira ntchito limodzi pokhala ndicholinga chimodzi chofaritsa Uthenga Wabwino. Mu nthawi ya Chipangano Chatsopano, uvangeli umapangidwa ndi okhulupirira omwe anabwera pamodzi ndicholinga chofuna kupititsa patsogolo Ufumu a Mulungu. Akhristu sanaiyanisidwe ndi mipingo yawo kapena kutanganidwa ndikulimbikitsa mipingo yawo kapena mabungwe awo. Tikuyenera kugwiririra ntchito limodzi ndicholinga chofuna kugwirisa bwino ntchito zipangizo zomwe ziripo kuti tikolole zokolola zauzimu zochuluka zomwe Mulugu analonjeza matsiku ano otsilidza. Muphunzira zambiri za uvangeli opangira pamodzi mu gawo la nkhumu ndi chisanu ya phunziroli.

### **PACHIMAKE PA KUBZALA MPINGO:**

Uvangeli wa Chipangano Chatsopano unapangisa kuti kuyambitsidwe misonkhano ya m'dera. Izi zimatchedwa kuti kuBzala mpingo. Ntchito ya uvangeli simakhala ya thunthu ngati okhukupirira atsopano zaznafike pokhala anthu odaririka mu Mpingo. Muphunzira



zambiri za kubzala mpingo mu gawo lachitatu la phunziroli pomwe mungaphunzire mwatsatanetsatane njira zomwe Paulo anagwiritsa ntchito. Mu Chipsngano Chatsopano otembenuka ntima anasinthidwa ndikukhala ophunzira monga mmene mpingo wa m'dera unaliri. Muphunzira zambiri za ndondomekoyi mu Mutu wa Khumi ndi Zitatu, “Zisankho Kapena Ophunzira.”

### **ZOTSATIRA ZA UMBONI**

Zotsatira za njira za uvangeri za Chipangano Chatsopanozi zinali zambiri.

**Ndipo dzanja la Ambuye linali nao; ndi unyinji wakukhulupira unatembenukira kwa Ambuye. (Macitidwe 11:21)**

Mpingo waung'ono waku Aefeso unatenga Uthenga Wabwino kupita nawo kwa mynthu aliyense yemwe amakhala ku Asia pa dzaka ziwiri zokha (Machitidwe 19:10). Gulu linanso longwa iri laku Atesalonika linalalikira dera lalikula la Greece (1 Atesalonika 1:8). Pomwe ophunzira anafika ku Atesalonika, zotsatira zambiri za kutumikira kwawo kunafupikitsidwa ndi akuluakulu achipembedzo omwe anati:

**...Omwe aja asanduliza dziko lokhalamo anthu, afika kunonso. (Macitidwe 17:6)**

Anatembenukiza dziko lonse, mu mdera loipa ndi losaopa Mulungu, popanda njira zofalitsira uthenga zamakono.

MAFUNSO OZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera.

---

---

2. Lembani mwachidule mfundo zofunikira za uvangeli wa Chipangano Chatsopano.

---

---

---

---

---

---

---

---

3. Kutotokozani zotsatira za uvangeli wa Chipangano Chatsopano

---

---

---

---

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

### ZOONJERERA POPHUNZIRA

1. Mwaphunzira muphunziroli kuti mu nthawi za Chipangano Chatsopano dzina nyumba iri yonse inali malo a uvangeli. Wonani zinthu zochitika zotsatirazi, zomwe zinachitikira ma nyumba:
  - Macitidwe 2: Mzimu Woyera unaperekedwa panthawi ya nkumano wamapephero muchipinda chapamwamba cha nyumba.
  - Macitidwe 5:42: Okhulupirira amapembeza mu kachisi ndi m'nyumba, ndipo amapita khomo ndi khomo kuyendera, kuyanjana ndiku lambira.
  - Machitidwe 8:3: Pamene Paulo anayesera kuti agonjese mpingo, sanangoyika mphamvu zake pama kachisi opepherera. Analowa nyumba ili yonse kuyesera kuti akalepherese kufalikira kwa Uthenga Wabwino. Nyumba izi mumachitikala mapephero.
  - Machitidwe 9:11,17: Paulo anaphunzitsidwa ndi Hananiya mu nyumba.
  - Machitidwe 10: Masophenya oyamba okafikira zikhalidwe zina kukudza Uthenga Wabwino anaperekedwa kwa Petro pamene anali kupephera m'nyumba.
  - Machitidwe 10: Uthenga woyamba kwa anthu amitundu unalalikiridwa m'nyumba.
  - Machitidwe 12: Nkumano wama pemphero omwe unachitika m'nyumba unapangisa kuti Petro akapulumusidwe kundende.
  - Machitidwe 20:20 ndi 28:30-31: Paulo anaphunzitsa pabwalo ndi nyumba munthawi yake ya utumiki.
  - Machitidwe 20:7-12: Paulo pamene amayankhula mu nyumba Utiko anagwa padzenera.
  - Machitidwe 21:8-14: Mabvumbulutso awu neneri amachitikira m'nyumba.
  - 1 Akorinto 16:19; Aroma 16:3-5; Ankolose 4:15; ndi Filemoni 1:2; amakamba za mipingo yam'nyumba.
2. Mafunso otsatirawa akunthandizirani kuti mukaganidzire njira zosiyana siyana zakufikira anthu polalikira. Zifunse ni nokha? kodi iyi ndi njira.” ...
  - Ya Baibulo: Njirazi zikuyenera kukhala zokhazikika pa malamulo omwe amakambidwa mu baibulo.
  - Zamphamvu: Njira zikuenera kukhala zopindulitsa. Chipambano chimawonetsera kuti anthu osapulunka awulandira bwino Uthenga Wabwino.
  - Zokwanira: Njira zikuenera kupereka magwiritsidwe abwino ku zinthu za uzimu monga kwa anthu, katundu ndi zachuma.
  - Zoenera kuchikhalidwe: Zomwe zimagwira mu dziko lina sizingakhale zoyenera mu dziko lina. Zomwe zimagwira ndi gulu lina a anthu zimatha kukanidwa ndi gulu lina.
3. Chitani maphunziro a Uthenga Wabwino mwa inu nokha, Macitidwe a Atunwi ndi Makalata. Kaziweni malamulo owonjedzera a kulalikira kwamu Chipangano Chatsopano ndi zitsanzo za malamulo zomwe zaphunzitsidwa mu phunziro iri.

## CHAPUTALA 8

### NJIRA: MAFANIZO A M'CHIPANGANO CHATSOPANO

#### ZOLINGA:

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba vesi yotsogolera.
- Tanthauzani mau akuti “fanizo”
- Kufotokoza chifukwa chimene Yesu amagwiritsira mafanizo.
- Kuzindikira mfundo za uvangeli mu mafanizo

#### VESI YOTSOGOLERA

**Ndipo ndi mafanizo otere ambiri analankhula nao mau, 1 monga anakhoza kumva. (Marko 4:33)**

#### CHIYAMBI

Mu phunziro langothali munaphunzira za njira za uvangeli za Chipangano Chatsopano. Pali mafanizo ambiri mu Chipangano Chatsopano omwe amaphunzitsa zambiri za ndondomeko za uvangeli. Fanizo ndi nkhani yomwe imagwirisa ntchito zitsanzo za chilengedwe pofuna kusonyeza chilungamo za uzimu. tanthauzo lenireni la mau oti “fanizo” ndi “kuyika pafupi, kuyerekeza.” Mu mafanizo, Yesu amayerekeza zitsanzo zinthu zachilengedwe ndi chlungamo chauzimu. Fanizo ndi nkhani ya pa dziko lapansi yomwe iri ndi tanthauzo lakumwamba.

Mu phunziro iri muphunzira mafanizo a Chipangano Chatsopano omwe amaphunzisa mfundo za uvangeli.

#### CHIFUKWA CHANI MAFANIZO?

Ophunzira anamufunsa Yesu chifukwa chimene anagwiritsa ntchito mafanizo akamaphunzisa chilungamo cha uzimu:

**Ndipo ophunzirawo anadza, nati kwa Iye, Cifukwa canji muphiphiritsira iwo m'mafanizo? (Mateyu 13:10)**

Yesu anayankha:

**Ndipo Iye anayankha nati, Cifukwa kwapatsidwa kwa inu kudziwa zinsinsi za Ufumu wa Kumwamba, koma sikunapatsidwa kwa iwo. (Mateyu 13:11)**

Kumvetsa kwa chilungamo cha uzimu chomwe chinaphunzidwa mu mafanizo chinapasidwa kwa ophunzira chifukwa iwo anali ndi malingaliro auzimu. Iwo omwe analibe malingaliro auzimu amanva mafanizo nalephera kumvetsesa. Chilungamo chauzimu chimamvetsetseka ndi malingaliro auzimu okha.

**Koma munthu wa cibadwidwe ca umunthu salandira za Mzimu wa Mulungu: pakuti aziyesa zopusa; ndipo sakhoza kuzizindikira, cifukwa ziyesedwa mwauzimu. (1 Akorinto 2:14)**

Munthu wamalingaliro auzimu ndi amene wabadwanso mwasopano mu uzimu. Iwo omwe ali ndi malingaliro auzimu ndi omwe amvetsetsa mafanizo. Iwo omwe ali ndi malingaliro aumunthu, auchimo sangamvetsetse.

## MAFANIZO A UVANGELI

Yesu anakamba mafanizo ambiri a uvangeli ndi kufotokozerwa mmene Ufumu wa Mulungu ongazafalitsidwire pa dziko lonse lapansi. Werengani mafanizo otsatirawa:

**Nkhosa yotayika: Mateyu 18:12-14; Luka 15:4-7**

**Ndalama yotayika: Luka 15:8-10**

**Mwana wolowerera: Luka 15:11-32**

Mafanizo awa akusonyeza chifundo cha Mulungu pa otayika ndi mmene mungawafunire modzipereka. Sizikutengera kuti atayika bwanji. Nkhosa inasochera kutali. Ndalama inatayika chifukwa chakusamala. Mwana anasochera chifukwa chakupanduka kwake. Mulungu sakukhuzidwa ndi m'mene anthu atayikira, koma kuti apedzeke. Mukuyenera kuyesayesa mwa njira ina iriyonse kuti mukapedze iwo omwe atayika mu uchimo. Mukuyenera kupita komwe iwo ali, osati kuwadikirira kuti iwo abwere kwa inu.

**Fanizo la phwando lalikuru: Luka 14:15-23**

Uvangeli sukuyenera kusiyidwa chifukwa anthu ena akukana kuyankha muyitano wa Uthenga Wabwino. Mukuyenera kusaka omwe ali ndi njara ya uzimu ndikuwabweresa ku phwando la uzimu lomwe lakonzedwa ndi Ambuye,

**Mkuyu wosabala: Luka 13:6-9**

Mkuyu umayimirira mtundi wa ana a Israyeli. Mulungu anaukitsa ntundu wa Israyeli ndicholinga choti mwa iwo adzabvumbulutse Ufumu wake ku dziko lonse lapansi. Mulungu anayesesa kuti “m’ntengo” wa Israyeli ubale zipaso pakati pa mayiko amitundu pakugawana nawo chidziwitso chomwe ali nacho cha Mulungu woota. Koma Israyeli anakhalabe osabereka. Ndipo Mulungu waukitsa Mpingo ndi cholinga ichi. Mulungu amatsamalira okhulupirira pofuna kuti awapange akhale obala zipatso, monga m'mene anachitira ndi mtundu wa Israyeli. Cholinga chake ndi chimodzi: Tikuyenera kubala “zipatso” kwa amitundu pakugawana nawo chidziwitso chatu cha Mulungu woota. Mulungu sasangalatsidwa ndi mitengo yomwe sibala zipatso.

**Matalente: Mateyu 25:14-30; Luka 19:11-27**

**Munthu wapaulengo wautali: Mariko 13:34-37**

**Akapolo: Mateyu 24:43-51; Luka 12:39-46**

**Kapolo wochezera: Luka 12:36-38**

**Kapitawo wokhulupirika: Mateyu 25:14-30**

Mafanizo a “akapolo” awa akutsindikidza za ukapitawo wanzeru wa Uthenga Wabwino waperekedwa kwa okhulupirira. Ookhulupirira wina aliyense wapatsidwa matalente kapena kuti luso lapaderadera kuti akagwsirise ntchito pofalitsa Uthenga Wabwino. Kaya luso lano ndiralikulu kapena ayi, mukuyenera kugwirisa ntchito zomwe Mulungu wakupatsani. Pamene Yesu anagadzabwerenso pano pa dziko lapansi, iwo omwe agwiritsa bwino ntchito luso lawo ndi omwe agadzalandire mphoto (Luka 16:10-12).

**Wofesa: Mateyu 13:3-8; Mariko 4:3-8; Luka 8:5-8**

Uthenga Wabwino umafalitsidwa pakufesa mbeu za Mau a Mulungu. Palibe kuchulukitsa ngati palibe Mau a Mulungu. Chipatso chimadalira moyo omwe ulinkati mwa mbeu (Mau a Mulungu) ndi malandiridwe a nthaka (momwe munthu akulandirira Mau a Mulungu). Pamakhala kalandiridwe kosiyanasiyana ka kufesa Mau.

Udindo wanu ndikufesa. Pomwe mukufesa Mau a Mulungu, nthaka ina ndiyokodzeka kubereka zokolola. Nthaka ina siyokodzeka kulandira ndipo imabereka zokolola zochepa. Ngakhale Yesu aakumana ndi nthaka zosakodzeka pa utumiki wake wa dziko lapansi:

**Ndipo kumeneko sanakhoza Iye kucita zamphamvu konse, koma kuti anaika manja ace pa anthu odwala owerengeka, nawaciritsa.**

**Ndipo anazizwa cifukwa ca kusakhulupirira kwao. Ndipo anayendayenda m'midzi yozungulirapo, naphunzitsa. (Marko 6:5-6)**

### **Namsongole ndi Tirigu: Mateyu 13:24-30**

Pomwe mukulalikirira okhulupirira atsopano amaonjezedw ku Mpingo, Satana amayesesa kugonjetsa ndondomekoyi. Amafesa anthu omwe akukambdwa kuti ndi “namsongole” pakati pa mbeu zabwino za Ufumu wa Mulungu. Anthu ena omwe amati ndi okhulupiriraomwe mabwera mu mpingo kudzera mu uvangeli si odzipereka. Ndi “anamsongole” omwe afesedwa ndi Satana. Yesu sakufuna kuti inu mudzitaya nthawi ndi mphanvu zanu pofuna kulekanitsa namsongole ndi tirigu. Pitolizani kufesa mbeu ndi kulalikirira. Pomwe Yesu akadzabweranso, namsongole adzalekanitsidwa pa nthawi yokolola.

### **Ngale la Khoka: Mateyu 13:47-50**

Yesu anayerekeza uvangeli ndi khoka loponyedwa m'nyanja. Mitundu yonse ya nsomba imalowamo, koma khoka ikakokedwa ku ntunda nsomba zabwino zimasiyanitsidwa ndi zoyipa. Ufumu wa Mulungu umakopa amuna ndi akadzi kuchokera ku mayiko onse. Ambiri amalowa. Ena mowona ntima, ena ayi. Pachiweruzo pamene Mulungu akadzakoka khoka, abwino ndi oyipa azatsiyantsidwa. Inu simunayitanidwe kuti mukatsiyantise, munayitanidwa kuti mukaweze.

### **Mbeu ya Mpiru: Mateyu 13:31-32; Mariko 4:31-32; Luka 13:19**

Ufumu wa Mulungu umachuluka ngati mbeu ya mpiru. Mbeu ya mpiri ndiyaying'ono kwambiri, koma kukhwima kwake umakhala ntengo waukulu. Ufumu wa Mulungu pa dziko lapansi unali ndi chiyambi chaching'ono. Pamene Yesu anapita kumwamba utatha utumiki wake wapadziko lapansi, anasiya ka gulu kocheha ka omutsatira kuti afalitse Uthenga Wabwino. Kagulu kameneko ka okhulupirira kachulukitsidwa kufikira zikwi zikwi za otsatira mu mayiko ambiri.

### **Chotupitsa Mikate: Mateyu 13:33; Luka 13:21**

Ngati Chotupisa mu nkate, Uthenga Wabwino umafalikira mu “mtanda” wonse wa dziko. Ngati chotupisa, mphanvu ya Ufumu sili ya kunjira koma nkati mwa munthu.

### **Mpesa Ndi Nthambi Zake: John 15:1-16**

Fanizo iri limafotokodza zaubale wa Yesu, ife ndi ndondomeko ya uvangeli. Iye ndi mpesa wa uzimu ndipo ife ndi nthambi. Sitingabale zipatso patokha. Timabala zipatso pokhapokha ngati tiri olumikizidwa ndi moyo wa mpesa, Yesu. Yesu akufuna kusadza moyo wanu chinachilichonse chomwe sichibala zipatso kuti mukabale zipatso zauzimu.

### **Zotuta: Mateyu 9:37-38; Luka 10:2**

Mu fanizo iri, munda ndi dziko. Zotuta ndi makamu a anthu omwe ari okonzeka kulandira Uthenga Wabwino. Kututa kwakukulu kukudikirira kukololedwa ndi ogwira ntchito auzimu a Mulungu.

## MFUNDO DZINA ZA UVANGELI

Yesu anaphunzisa mfundo dzina za uvangeli machidule:

### **Kuunika kwa Dziko: Mateyu 5:14-16; Luka 8:18**

Uthenga Wabwino ufalikira pomwe okhulupirira angaonekere ngati kuunika kuchokera ku mudzi okhazikika pamwamba pa phiri omwe umaonedwa kuchokera patali. Tikuyenera kubwera kuunika kwa dziko (Yesu) ku dziko lomwe ladzadza ndi mdima wa uzimu.

### **Mchere wa Dziko: Luka 14:34**

Mu nthawi Bukhu Lopatulika, mchere umatikitidwa pa nyama kuti isawole. Okhulupirira ndi mchere omwe wapakidwa pa dziko ndi uthenga woteteza (chipulumutso) womwe ungapulumutse ku kuwola (imfa yauzimu) kwa tchimo.

### **Chuma cha m'Mwamba: Mateyu 6:19-21; Luka 12:15**

Okhulupirira sakuyenera kukhuzidwandi chuma cha dziko lapansi. Pomwe tikufalitsa Uthenga Wabwino, timasunga chuma chauzimu ku Mwamba.

### **Chipata Chotakata: Mateyu 7:22**

Simungaweruze njira yabwino potengera **words omitted**. Njira yaku Gehena imakopa anthu ambiri pomwe njira yaku moyo wosatha imapezedwa ndi anthu ochepa chabe.

### **Ntchito Zambiri: Mateyu 7:22**

Ntchito zambiri zodabwitsa zizapangidwa ndi anthu ena. Koma kuchita ntchitozi sizitanthauza kuti mukuchita chifuniro cha Mulungu ndi kukwanirisa cholinga Chake. Ntchito za Mulungu zikuyenera kugwiridwa ndi anthu ake mu njira ake.

### **Pang'ono ndi Kwambiri: Mateyu 10:42; Mateyu 14:15-21**

Chinachirichonse chochitika mu dzina la Yesu, ngakhale chimene chikuoneka chaching'ono, ndi zaphingu. Chozizwa cha mikate ndi nsomba ikusonyeza m'mene Mulungu amachulukitsira ndi kugwirisa ntchito zochepa zomwe tikakwanise kupereka. Izi ndi zoonazizeni za chidwi chochepa pa uvangeli.

### **Kukula Kumafuna Kusintha: Marko 2:21-22; 7:13**

Kukula kwatsopano kumafuna kusintha. Inu simungayika zinthu zatsopano mu zotengera zakale za makolo ndi moyo wauchimo. Kuthekera kwamphanvu kwa Uthenga wabwino kumabisidwa ndi anthu omwe amagwiritsitsa ku zikhalidwe zamakolo ndi kukana kusintha.

### **Kupeza Phindu pa Kuluza: Marko 8:34-37; 10:29-30**

### **Kulandira pa Kupereka: Luka 6:38**

Mfundo za dziko lapansi zimati munthu amapindura akamapeza zochuluka. Yesu anaphunzisa kuti umapindula kwambiri ukaluza chirichonse. Zomwe zimaoneka ngati kutaya mu dziko lakuthupi ndikupindula kwakukulu mu dziko la uzimu. pamene mukuzipereka ku ntchito ya uvangeli, muzapedza mphoto za muyaya.

### **Imfa imaberetsa Moyo: Yohane 12:24**

Kuti mukhale ophunzira obala zipatso mukuyenera kufa kudzilakolako za thupi. Mukuyenera kufa ku tchimo ndi kutsiya njira dzanu ndikuyamba kutsata Yesu pakukolola zotuta za uzimu.

## MWACHIDURE

Poyerekezera ndi uvangeli, chiphunziso cha Yesu chikuonetsa kuti sasangalatsidwa ndi:

- Usozi osagwira nsomba.
- Phwando lopanda anthu
- Kufesa koma osakolola.
- Ntengo omwe sukubala zipatso
- Nkhosa yotayika yomwe sinabweretsedwe mu khola.
- Ndalama yotayika yoyang'anidwa koma osapezeka.
- Akapolo osabala zipatso.
- Nthaka ya uzimu yosabala zipatso.
- Zokolola zakucha koma zosakololedwa.

Atate wathu, yemwe sakufuna kuti ingakhale moyo umodi uwonongeke, ndiwachidwi ndi zosatira za uvangeli.

**Ambuye sazengereza nalo lonjezano, monga ena aciyesa cizengerezo; komatu aleza mtima kwa inu, wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa. (2 Petro 3:9)**



## MAFUNSO OZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera.

---

---

2. Tanthauzirani mawu oti “fanizo.”

---

---

3. Kodi ndichifukwa chani Yesu amagwiritsa mafinizo pophunzisa omutsatira?

---

---

4. Mwachidule fotokozani mfundo za uvangeli zaphunzisdwa muma fanizo omwe ali mmunsiwa:

Phwando lalikuru

Mkuyu wosabala

Mwana, Nkhosa, ndi Ndalama Yotayika:

Wofesa

Namsongole ndi Tirigu

Ngale la Khoka:

Mbewu ya Mpiru:

Chotupitsa Mikate:

Mpesa Ndi Nthambi Zake:

Zotuta:

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

## ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Pitirizani maphunziro anu mfundo za uvangeli zomwe zawonetseredwa muma fanizo amu Chipangano Chatsopano. Gwiritsani ntchito zitsanzo zomwe zaperekedwa muphunziroli paku phunzira fanizo liri lonse la Yesu mwakuveka bwino. Kodi mungazindikire mfundo zoonjezera za uvangeli?

2. Ziwunikire nokha moyo wanu molingana ndi ziphunzitso za uvangeli pama fanizo omwe anenedwawa:

-Kodi mukuwedza popanda kugwira?

---

-Kodi mukubzala popanda kukolola?

---

-Kodi muli ngati mtengo osabala zipanso?

---

-Kodi mukusaka saka khosa yoatayika?

---

-Kodi ndinu kapolo wobereka ziatso?

---

-Kodi dothi lomwe mukugwirapo ntchito ndila chonde?

---

-Kuti mukulengapo nawo gawo pa kukolola monga kututa muuzimu mu dera lanu? Dziko lanu? Dziko lapansi?

---

## **CHAPUTALA 9**

### **NJIRA: UVANGELI WA PANOKHA**

#### **ZOLINGA**

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba vesi yotsogolera.
- Tanthauzani wa panokha
- kulemba njira zitatu za uvangeli wa panokha
- kufotokoza m'mene mungatengere moyo kwa Khristu

#### **VESI YOTSOGOLERA**

**...Asamariya ambiri anamkhulupirira iye cifukwa ca mau a mkazi, wocita umboniyo, kuti, Anandiuza ine zinthu ziri zonse ndinazicita. (Yohane 4:39)**

#### **CHIYAMBI**

Mwaphunzira kuti njira zogawira Uthenga Wabwino za Chipangano Chatsopano zikuphatikiza uvangeli wa panokha ndi uvangeli wapagulu. Mu phunziro iri muphunzira mmene mungachitire uvangeli wa panokha. Mu Mutu Khumi mudzaphunzira mmene mungathanire ndi zophinja mungakumane nazo pamene mukupanga uvangeli wa panokha.

#### **UVANGELI WA PANOKHA**

Uvangeli wa panokha uli mmene dzina lake lionetsera. Ndikugawana Uthenga Wabwino pa iwe wekha ndi munthu modzi modzi. Uli uvangeli wakwa munthu ku munthu, modzi ku modzi. Uvangeli wa panokha umachitika mu njira zotsatirazi:

#### **KUCHITIRA UMBONI MWA CHETE**

Inu ndinu ochitira umboni mwa chete Uthenga Wabwino ndi mmene mumakhalira m'moyo. Moyo wanu ndi umboni wachinachake, kaya modzindikira kapena ayi. Ngati makhalidwe anu sagwirizana ndi umboni wanu wapakamwa wa Uthenga Wabwino, zimalepheretsa kuti anthu atsalandire chipulumutso.

Ingakhale machitidwe achi Khristu ndi umboni wamphanvu waka chetechete, anthu ambiri amavala zinthu zodzikongoletsera “zachipembezo” kapena kupachika mavesi a m'Baibulo m'manyumba mwawo, m'malo awo ochitira malonda, kapena mu galimoto. Nthawi zina zinthu izi zimatsogolera ku umboni wa mau pomwe munthu wosapulumuka akafunsa za zimenezi.

#### **TIMATHIRAKITI TA UTHENGA WABWINO**

Timathirakiti ta Uthenga Wabwino ndi uthenga wachidule wa Mau a Mulungu omwe nthawi zambiri umasindikidzidwa pa mapepala ang'onoang'ono. Si ta ntengo wapatali komanso osalempera kwambiri, zomwe zimapangisa kuti mathirakiti ambire agawidwe mosavuta kwa anthu omwe mungakumane nawo.

Mutha kupereka timathirakiti ta Uthenga Wabwino kwa aliyense, omwe mumachita nawo malonda limodzi, abwenzi, achibale, ingakhale anthu omwe mwangokumana nawo mu nsewu. Mutha kutiyika mu makalata omwe mumalemba ndi kuwasiya mu malo owerengera

mabuku, malo odyera, ndi malo ogwirirako ntchito. Komanso mutha kuwasiya mu basi, sitima za pantunda, olo malo okwererapo ndege.

Mukapareka thirakiti ya Uthenga Wabwino kwa munthu wina mudzinena kuti, “nachi chinachake chabwino kuwerenga” kapena “nachi chinthu chomwe chinasintha moyo wanga ndipo ndikufuna kugawana nanu.” Kalankhulidwe ngati aka nthawi zambiri kamatengera anthu ku umboni wa mau.

Pomwe mukusankha timathirakiti pofuna kuchita uvangeli wa panokha, muganizire mafunso ali munsiwa:

1. Kodi timathirakiti tikuyankha funso lomwe likufunsidwadi? Ngati likuyankhadi, anthu akhala ndi chidwi choti awerenge.
2. Kodi kalembedwa mwachidule? Likuyenera kulembedwa mwachidule komanso mwachindunji kapena anthu atopa kuwerenga asanamalize nkomwe.
3. Kodi tikukamba zabwino koma osatsutsa zikhulupiriro zina?
4. Kodi tikugwirisa ntchito zilankhulo za chipembezo zomwe munthu osapulumuka angavesese?
5. Kodi tasindikidzidwa mokuti titha kuwerengedwa mosavuta?
6. Kodi kathirakitiko kakugawa cholinga chenicheni cha Uthenga Wabwino?
7. Kodi kakupereka mwayi woti anthu avomereze ndikulandira Yesu Khristu ngati mpulumutsi?

Mulembe dzina lanu, komwe mumakhala ndi nambala yanu ya lanya pamalo pena pa mathirakitiwo kuchitira kuti munthu akafuna chithandidzo chapaderadera cha uzimu athe kulumikidzana nanu. Timathirakiti ta Uthenga Wabwino tomwe tikupangidwa masiku ano tambiri tikumakhala ndi malo oti mulembepo izi. Timathirakiti ta Uthenga Wabwino sitikutenga malo a umboni wa mau, koma tikungothandidzira chabe. Ubwino wake wa timathirakiti ndilakuti timapitiriza kuchitira umboni pomwe inu mwachokako.

## **UMBONI WA MAWU**

Ingakhale kuchitira umboni mwa kachetechete komanso kugawa timathirakiti ta Uthenga Wabwino ndi zopindura kwambiri, mukumbukire kuti izi si zonse zimene ntchito ya utumiki wawukulu imafuna. Imafuna kuti mugawe Uthenga Wabwino ndi mau. Umboni wa mau mu uvangeli wa panokha umasiyana ndi kulalikirira kapana kuphunzisa mu kachisi. Utha kumachitika makuyenda khomo ndi khomo kugawa Uthenga Wabwino. Utha kumachitikira ku malo osungiramo anthu okalamba, ku zipatala, ku ndende, malo ophunzirirako, malo amalonda, ndi malo ena ali onse omwe uvangeli ukuchikirirako. Munthu kugawana Uthenga Wabwino ndi abwenzi anu, achibale ndi omwe mumachita nawo limodzi malonda. Mutha kuchita uvangeli wa panokha pokhala opereka uphungu pamalo omwe pakuchitikira msokhano wachitsitsimutso komanso ngati wogwira ntchito pa gome mu mpingo mwamu. Mu uvaneli wa panokha, mutha kugawa Uthenga Wabwino ndi wina aliyense yemwe mwakumana naye.

Uvangeli wa panokha utha kuchitika mu njira yofunsa mafunso, ngati m'mene Yesu anachitira ndi mkazi pa chitsime pa Yohane 4. Mutha kukhazikika pa chinachake chimene chomwe mwachiona munthu akuchita kapena chotsowa chimene mwaona kuti akufuna. Mutha kuwafunsa mafunso omwe angakutengereni kuti mugawane nawo Uthenga wabwino.

Uvangeli wa panokha utha kuchitika pomwe mukuperekera umboni wa zomwe Yesu wachita pa moyo wanu. Pa Yohane 4, mkazi waku Samaliya anabwerera ku mudzi ndikukugawa zomwe wakumana nadzo. Izi zinapangitsa kuti anthu ambiri abwere ndikukumana ndi Yesu ndi kunva Uthenga Wabwino. Malembo akuti:

**...Asamariya ambiri anamkhulupirira iye cifukwa ca mau a mkazi, wocita umboniyo, kuti, Anandiuza ine zinthu ziri zonse ndinazicita. (Yohane 4:39)**

Umboni wa mkaziwo unali waufupi, chifukwa samadziwa zambiri za Ambuye. Iye anangoti, “Anandiuza ine zinthu ziri zonse ndinazichita.” Zomwe anaziziwa za Ambuye zinali chilungamo kwa iye. Chinali chidziwitso chomwe iye anamva yekha ndipo Mulungu anagwiritsa tchito mau ake.

Mulungu amadalitsa umboni wogwededzeka wa okhulupirira atsopano omwe akudziwa chowe iwo akulankhula kupotsa ma uthenga a anthu omwe akulalikira zinthu zomwe iye mwini sakuzimvesa bwino ingakhale ziri zinthu zoonza ndithu.

Kuchitira umboni wa m'mene munamudziwira Yesu ndi m'mene aliri kwa inu ndi njiri ya mphamvu kwambiri ya uvangeli. Umboni wanu umawonetsera Yesu mu malembo a m'Baibulo, kuchoka mu chipembedzo ndi mipingo, ndi kuwonetsa Kuti Yesu ndi wamoyo ndipo akadali kuchitachita matsiko ano. Anthu atha kunyozera Baibulo kapena chipembezo, koma sangakane zenizeni za zoonza zomwe zinachitikira inu.

Ngati mukuchita mantha ndikuperekera umboni wanu, ndizofunikira kuwulemba ndi kuwuwerepa pa inu nokha musanagawane ndi athu ena. Awa ndi amfunso omwe mukuyenera kuganidzira pomwe mukukonza umboni wanu:

- Kodi ndi chani chomwe chinakupangisana kuyamba kuganizira za Mulungu?
- Kodi Yesu munamudziwa bwanji?
- Kodi kumudziwa Yesu kwasintha chani pa moyo wanu?
- Kodi kwasintha chani pa banja lanu?
- Moyo wanu wasintha bwanji?
- Kodi chinthu chomwe chiri chozizwitsa chomwe chachitika ndi chani?

(Mwachinsanzo, kodi mwachiritsidwa or mwamasulidwa ku mankhwala ozungudza umbongo kapena mowa)

Mukamalidza kulemba umboni wanu, choyamba mugawane kaye ndi abwenzi anu a Chikristu. Muwafunse ngati pangakhale zosintha zomwe zingathandidzire kukopa osakhulupirira kwa Ambuye. Kenako uwerengeni pafupi pafupi mpaka mufike poti simungayang'anenso pomwe mwalembapo.

Uvangeli wa panokha uthanso kuphatikidza kugawana nyimbo ndi anthu ena. Davide anati:

**Ndipo anapatsa Nyimbo yatsopano m'kamwa mwdanga, cilemekezo ca kwa Mulungu wanga; Ambiri adzaciona, nadzaopa, Ndipo adzakhulupirira Yehova. (Masalmo 40:3)**

Monga mwa vesi iyi, nyimbo yolemekeza Mulungu ndi umboni omwe ungapangitse kuti anthu ambiri apulumutsidwe.

### **M'MENE MUNGATSOGOLERE WINA KWA KHRISTU**

Cholinga cha uvangeli wa panokha ndikutsogolera amuna ndi akazi, anyamata ndi atsikana, kuti apemphe kukhulukidwa kwa machimo ndikulandira Ambuye Yesu Khristu ngati Mpulumutsi. Pakutha pa nthawi, njira zotsogolera ena kwa Yesu zakonzedwa zomwe zimagwirisa ntchito mfundo ndi njira zosiyanasiyana pakugawa Uthenga Wabwino.

Pomwe chikonzero ichi chitha kukhala chopindula, njira imodzi ya uvangeli wa panokha singawiritsidwe ntchito nthawi zonse. Munthu aliyense yemwe mukumuchitira umboni ndi

wosiyana ndi nzake, ndizosowa zosiyana ndi mavuto osiyana. Kusiyanaku kumapangaisa kuti njira zosiyananso zizigwiritsidwa ntchito osati kumangogwirisa ntchito njira imodzimodzi nthawi zonse. Mukuyenera kukhala omvesera Mzimu Woyera, pakuti ndiamene amabweresa anthu ku chipulumutso. Amadziwa chenicheni chomwe munthu yemwe mukumuchitira umboni akusowa, pakuti amadziwa mitima ya anthu.

Chinthu chimodzi chomwe anthu onse osapulumuka ali nacho chofanana, ndi tchimo ndi kufuna Mpulumusi. Chifukwa cha ichi, osatengera ndi m'mene Mzimu Woyera angakutsogolereni kuti mukagawe Uthenga Wabwino, umbuni wanu ukuyenera kukhala olunjika pa cholinga chotsogolera ena kwa Khristu.

Kuti mukakwaniritse izi, kaonetsedwe ka umboni wanu kakuyenera kukhala ndi izi:

**KUONETSA: UTHENGA WENIWENI WA UTHENGA WABWINO:**

**KUPEREKA: ZOLINGA ZA UTHENGA WABWINO**

Onanitso Mutu wachitatu wa phunziroti omwe ukukamba za uthenga wa uvangeli. Zolinga zenizeni za Uthenga Wabwino zaperekedwa ndi Paulo pa 1 Akorinto 15:1-4. Onanitso ndimeyi mu Baibulo lanu. Uthenga ndi wakuti anthu onse kulikonse ndi ochimwa, Yesu anafera zoipa zathu, Anayikidwa m'manda, ndipo anauka kwa akufa malingani ndi malembo.

Awa ndi mavesi omwe angakuthandizeni pa kupereka Uthenga Wabwino:

-Mulungu ndi Mulungu woyera:

1 Petulo 1:16; Habakuku 1:13

-Chifukwa ndi woyera, tchimo linalekanitsa anthu ndi Mulungu:

Yesaya 59:2

-Tchimo ndi la dziko lonse; Anthu onse achimwa:

Aroma 3:10-12,23

-Mphoto ya tchimo ndi imfa:

Ezekieli 18:20; Aroma 6:23; Masalimo 9:17

- Mulungu siofuna kuti wina aliyense awonongeke:

1 Petulo 3:9; Yohane 3:16; Aroma 5:8

-Kuti apereke chipulumutso kwa anthu onse, Mulungu anapereka n nsembe yookwanira anthu onse:

Ahebri 10:10; Yohane 1:29; Agalatiya 2:20

-Yesu anatenga mphoto ya uchimo pomwe anafera pa mtanda:

1 Petulo 2:24; Yesaya 53:6,10

-Chipulumutso chaperekedwa kwa anthu onse:

1 Timoteo 2:4

-Lamulo lakulapa ndi la anthu onse:

Machitidwe 17:30

-Ochimwa akuyenera kuti alape ndi kulanfira Yesu kuti apindule ndi nsembe ya tchimo:

Yohane 1:12; 5:24

**KUTSEKA: KUITANA NDI KUYANKHA:**

Pomwe mukugawa Uthenga Wabwino, atengereni anthu osapulumuka ku mapangano ang'onoang'ono. Izi zitha kuchitita pakufunsa mafunso ngati awa:

-Kodi mukuganiza chani?

-Kodi munaganizirako...?

- Kodi mukuganiza kuti anthu amamva kuti...?
- Kodi mukuganiza kuti izi ndi zachilenda?
- Kodi izi zinakuchitikiraniponi?
- Kodi munakhalapo ndi vuto limenero?

Muonetsetse kuti akutenga nawo gawo pazokambiranazi. Mupereka mfondo zochepa, kenako muyambe kufunsa mafunso omwe angayitane mayankho. Yesu anagwiritsa ntchito njira iyi ndi mkazi pa chitsime pa Yohane 4 ndi Nikodemo pa Yohane 3.

Kugawa Uthenga Wabwino popanda kupereka mwayi kuti anthu avomereze ndi kupereka umboni chabe, koma osati uvangeli. Tinayitanidwa kuti tikapindule, osati kungopereka umboni. Mutseke kaperekedwe kanu ka Uthenga Wabwino ndikufunsa mafunso ngati awa:

1. “Kodi mwamvetsetsa zomwe ndi makuuzani?” Izi zimapereka mwayi woyankha funso linaliririronse ndi zolinga ndi kukhutira kuti amvetsetsa musanawalandiritse Yesu.
- 2.
3. “Kodi ndinu okondwa kulandira Yesu Khristu kukhala Ambuye ndi Mpulumutsi?” Mutsogolereni munthuyo mu pemphero lopempha chikhululukiro cha machimo ndi kuvomereza Yesu Khristu ngati Mpulumutsi.

Nthawi zonse muzindindire kuti pa uvangeli wa modzi modzi mukupanga zoposa kungogulitsa malonda kapena kupititsa patsogolo mpingo. Mukuchita ndi tsogolo losatha la miyoyo. Kulowa mu Ufumu wa Mulungu ndizofanana ndi muyitano wa ukwati, ngati mmene Yesu anawonetsera mu fanizo la phwando la ukwati pa Mateyu 22:2-5. Iwo omwe avomereza muitano ndi amene amalowa. Sizokwanira kungonena kuti, “ndikuganizira kupezeka.”

Pamene Yesu ananena ku ophunzira ake’ “Nditsateni ine, ndipo ndizakupangani kukhala asodzi a anthu” (Mateyu 4:19), amapereka chitsanzo chakuthupi cha zoonadi za uzimu. palibe nsodzi yemwe amangoponya khoka lake. Amalikokaso ndicholinga choti akole nsomba.

### **KUYENDERA: KUMPHUNZISA:**

Mu utumiki waukulu omwe walembedwa pa Mateyu 28:19-20, pali mitundu iwiri ya ziphunziso zomwe zalembedwa. Choyamba ndikugawa Uthenga Wabwino womwe ungawatsogoze anthu ku chipulumutso. Chachiwiri ndi kuphunzitsa obadwa watsopano atatha kulandira Yesu. Uvangeli (mtundu woyamba wa chiphunziso) ulibe chidzalo popanda kuphunzisa (kutsatira).

One otembenuka atsopano akuyenera kuyenderedwa atatha kulandira Yesu Khristu ngati Mpulumutsi wamoyo wawo. Muphunzira zambiri za kuyendera mu Chaputala 13.

MAFUNSO OZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera.

---

---

2. Tanthauzirani uvangeli wapnokha.

---

---

3. Lembani njira zitatu zomwe uvangeli wa modzi modzi umachitikira.

---

---

4. Fotokozani mmene mungamutsogolerere munthu kwa Khristu.

---

---

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)



## ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Anthu osapuluma ambiri amakhala mayiko amene ayandikirana ndi kulalikirira kwa chikhalidwe. Olalikira obwera samapatsidwa ma viza ndipo sikungakhala kotheke kukalalikirira pagulu, chitsitsimutso Uthenga Wabwino kapena zochitika zina.

Mumayiko amenewa, kalilikira modzi mozi kofunikira kwambiri. Njira imodzi yomwe okhulupirira amalalikira mayiko amenewa ndipogwiritsa “nctito yomanga mahema” Mwaphunzira kale mene Tumwi Paulo amagwirira ntchito kuti akazithandize yekha kudzera kuntchito yake yopanga ma hema.

Mayiko amene ali kufipi ndi kulalikirira kwa chikhalidwe, okhulupirira akulowa ndi ma viza ogwirira ntchito, kupedza ntchito kuti akazithandize okha, ndipo kenako kugawana Uthenga Wabwino ndi anthu amene awazungulira. Ngakhale okhulupirira amenewa akugwira ntchito yachikunja, cholinga chawo chenicheni ndikulalikirira kwa modzi modzi. Njira yogawana Uthenga Wabwino imatchedwa “kumanga ma hema”

2. Pamene mukupanga utumiki wa munthu modzi modzi, mukuenera kukhala osamalitsa pogwiritsa ntchito mau achipembedza kapena fundo zoti munthu osapuluma sangathe kuvetsesa. Izi zitha kukhala. “Opulumutsidwa, obadwa mwatsopano, odzadza ndi Mzimu Woyera, Akristu, halleluya” ndizina zambiri. Mawu awa ndiwodziwika kwambiri kwa okhulupiriranu, koma kwa otsapulumsidwa samatha kuwavesesa.
3. Mu utumiki wa modzi modzi, musachite manyazi kugawana Uthenga Wabwino ndi ana. Perekani kachitsanzo kophweka zokhuzana ndi Uthenga Wabwino. Ngati angathe kuvesesa izi, afuseni mene akuvera kenako alandiritseni Yesu.
4. Mutha kusitha machedzedwe ana kukhala mwayi oti mugawane Uthenga Wabwino. Awa ndimaganzo ena:

\*\*\*

Pamene wina wafunsa: “Ungandiuzeko kuti nthawi ili bwani?”

Yankho: “Malingana ndi wontchi yangayi kapena mu baibulo?”

Pitiridzani kuchedza: Awunzeni nthawi yeniyeniyeni, komanso gawani kuti baibuloso imakamba za nthawi. Imanena kuti ndi nthawi yamene samudziwa Ambuye alape ndikubwera kwa Iye.

\*\*\*

Wina akafunsa: “Chatsopano ndi chani?”

Yankho: “Ndikhani yanji mukufuna kumva? Yabwino kapena yoipa?”

Pitiridzani kuchedza: Yankho lawo likhala kuti “nkhani yabwino” --- ndiye gawanani nthawi ya bwino ya Uthenga Wabwino.

\*\*\*

Pamene wina wakugundani mwangozi ndie ndikunena kuti “pepani.”

Yankho: “Otsadandaula. Ngozi imachitika. Kapena mwina siyinali ngozi”

Pitiridzani kuchedza: “Mwina izi zinakodzedwa kuti zikachitike kuti ndikathe kugawana nanu chinthu chatengo watali ndi inu”

\*\*\*

Ngati ogulitsa katundu wakupasani ndalama zanu zambiri, bwezani ndalama ndikunena kuti: “Munandibwedzera ndalama zambiri.”

Pitiridzani kuchedza: “Panali nthawi yina yake m’moyo mwanga imene ndinkasunga ndalamayi, koma pamene ndinakhala Kristu zinthu zinasitha.? Kenako gawanani men Uthenga Wabwino watsithira moyo wanu.”

\*\*\*

Pamene ogulitsa katundu wakufunsa kuti: “Ndikuthandizeni?”

Yankho: “Eya, koma ngatiso inu mungandilore kuti ndikuthandizeni pamapeto pake.”

Pitiridzani kuchedza: Ogulitsa katundu akufusani kuti “Ungandithandize chani?” awuzeni!

\*\*\*

Pamene munthu wakufunsani kuti akufuna moto ayasire foday, nenani: “Sindimagiwiritsa ntchito chichitikireni chivomeredzi.”

Pitiridzani kuchedza: ndizachidziwikire kuti munthuyo afuna kuti, “Chibvomeredzi chanji?”

Yankho, “Chimene chinachitika m’moyo mwanga pamene ndinakhala Nkhristu.”

\*\*\*

Pamene mwayakha lamya ndipo munthuyo akudzati: “Pepani, ndayimba nambala yolakwika.”

Yankho: “Ayi, munayimbana nambala yolondola.”

Pitiridzani kuchedza: akanena kuti, “Mukutathauza chani?” awuzeni kuti mwina izi zachitika kuti akapasidwe mwayi oti akave chinthu chomwe chingasithe moyo wawo ndi tsogolo lawo lamuyaya.

\*\*\*

Kodi mungaganize mwayi wina odabwitsa kuti kufikira tsiku ndi tsiku kutha kuchita pakugawana Uthenga Wabwino? Ganizani izi: kodzani mayakho mwa inu nokha, ndipo mukakozekere kuwagwiritsa ntchito.

Nthawi ili yonse mukakumbukire, mwina, kuti mafikiridwe ena siabwino munyengo iliyonse. Nkhani oseguka kuti Mzimu Woyera akusogolereni. Kufikira kwake kumakhala kolondola tsiku liri lonse!

5. Mukavetsetsa ubwino wa ulaliki wa modzi modzi pamene mukalingalire zinthu izi:

-Tsokhani wawukulu ndiwofunikira, koma anthu ambiri otsapuluma sabwera kuzavera olalikira. Palibe alaliki okwanira kuntchitoyi, ndipo pali mayiko ambiri kumene njira iyi simaloledwa chifukwa cha malamulo aboma.

-Kulalikirira pa nyumba yowulusa mau ndichamphamvu, koma anthu ambiri adziko lapansi alibe ma wailesi. Pamene boma lomwe siligwirizana ndi zauchi Kristu likulamulira, amachoseratu zimenezi.

-Kulalikirira pakanema ndichamphamvu, koma anthu ambiri adziko lapansi alibe makanema owonera. Pamene boma lomwe siligwirizana ndi zauchi Kristu likulamulira, amachoseratu zimenezi.

-kulalikirira kogawa galamukani kuli ndi malo ake, koma anthu ambiri samatha kuwerenga, kulibe mabukhu okwanira, ndipo siringakwanitse kupititsa mabukhu achi Kristu kumayiko ena.

-Kulalikirira nyumba ya mpingo yomwe imakhala ndi malo ake, ambiri alibe nyumba ya mpingo. Palibe nthawi kapena ndalama kuti mukamangene nyumba yokwanira kukalalikirira dziko lonse ndi njira iyi. Nyumba za mpingo ndizosaloredwa mayiko ambiri.

Njira zomwe zakulalikirira kuziphatikidza sizingalalikire dziko lonse popanda kulalikirira kwa modzi modzi.

6. Phunzirani uvangeli wa modzi modzi omwe unachitika ndi Yesu:

-Andreya, Yohane ndi Petro:	Yohane 1:35-45
-Filipi ndi Natanayeli:	Yohane 1:43-51
-Nikodemo:	Yohane 3
-Mkadzi waku Samariya:	Yohane 4
-Mkulu wina:	Yohane 4:46-54
-Kuyitanidwa kwa Simoni } Andreya ndi Yakobo }	Luka 5:1-11
-Wakhate:	Marko 1:40-45
-Wanjenje wonjamulidwa Ndi azake:	Marko 2:1-12
-Mayitanidwe a Mateyu:	Marko 2:13-17
-Wopuwala ku thamanda la Betesda:	Yohane 5
-Munthu wa dzanja Lopuwala:	Luka 6:6-10
-Kenturiyo:	Luka 7:1-10
-Mkadzi wamasiye waku Nayini:	Luka 7:11-17
-Mkadzi ochimwa munyumba	

Ya Simoni Mfarisi:	Luka 7:36-50
-Wamzimu wonyasa ku	
Gerasa:	Marko 5:1-20
-Yairo ndi banja lake:	Marko 5:21-43
-Mkadzi wavuto la mwadzi:	Marko 5:25-34
-Akhungu awiri:	Mateyu 9:27-31
-Chiwanda chosalakhula:	Mateyu 9:32-34
-Mkadzi waku kanani:	Mateyu 15:32-
-Munthu usalakhula ndi	
Osava:	Marko 7:32-37
-Wakhungu waku	
Betesda:	Marko 8:22-26
-Mwana waziwanda:	Marko 9:14-29
-Zimayi ogwida ndi	
Chigololo:	Yohane 8:1-11
-Ophunzira atatu:	Luka 9:51-62
-Wacilamulo:	Luka 10:25-37
-Munthu obadwa ndi	
Khungu:	Yohane 9
-Mkadzi wopetekaa:	Luka 13:10-21
-Munthu mwini Cuma:	Mateyu 19:16-22
-Akhungu aku Yeriko:	Marko 10:46-52
-Zakeyu:	Luka 10:1-10
-Yudasi Isikaliyoti:	Luka 22; Yohane 13; Mateyu 27
-Pilato: Yohane	18-19; Luka 23
-Herodi:	Luka 23; Marko 15
-Okuba awiri;	Luka 23:32-43

#### 7. Phunzirani ma utumiki a modzi modzi mu Macitidwe a Atumwi:

-Petro ndi Yohane ndi munthu	
Wopunduka:	3:1-11
-Filipi ndi Simoni Wamatsenga:	8:9-24
-Filipi ndi mdindo:	8:26-40
-Hananiya ndi Saulo:	9:10-20
-Petro, Eneya ndi Dorika:	9:32-42
-Petro ndi Korneliyo:	10:1-11, 18
-Paulo ndi Elima:	13:6-12
-Barnaba ndi Paulo Sergio:	13:7-12
-Paulo ndi Sila, Lidia:	16:12-15
-Utumiki wa Paulo ku Efeso	
Wa nyumba ndi nyuma:	20:17-35
-Paulo, Felike ndi Drusila:	24:24-27
-Paulo ndi mfumu Agripa:	26:1-
-Paulo, Popliyo ndi tate	
Wace:	28:7-11
-Paulo munyumba yake yaku	
Roma:	28:16-31

## CHAPUTALA 10

### NJIRA: KUTHANA NDI ZOVUTA

#### ZOLINGA:

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba ma vesi otsogolera
- Kufotokoza chifukwa chimene anthu amawiringula
- Kuthana ndi zovuta zomwe zimaza pa munthu akamatumikira

#### VESI YOTSOGOLERA:

**Pakuti chilengedwere dziko lapansi zaoneka bwino zosaoneka zace ndizo mphamvu yace yosatha ndi umulungu wace; popeza zazindikirika ndi zinthu zolengedwa, kuti iwo adzakhale opanda mau akuwirungula. (Aroma 1:20)**

#### CHIYAMBI

Phunziro iri likuthandizirani mmene mungathanire ndi nyengo yovuta imene mungakumane nayo pa uvangeli. Ndizosatheka kuthana ndi nyengo zonse zovuta zomwe muli nazo, koma takhazikika kwambiri pa mavuto omwe amachitikachitika.

Kumbukirani kuti awa ndima ganinzo chabe amene mungathanire ndizovuta kuchokera kwa anthu amene anagwirapo ntchito ya uvangeli. Ndichinthu chofunika kwambiri kudalira pa mphamvu ya Mzimu Woyera munyengo zowawa, kuchita izi ndichithu chamtengo wapatali.

#### KUMVETSA CHIFUKWA CHIMENE ANTHU AMAWIRINGULA

Ndizinthu zothandiza kwambiri kuziwa zifukwa zimene anthu amawiringula kapena kupereka zodandaula pa uvangeli. Nthawi zina satana amayika mafunso kapena zowiringula mumaganizo a munthu. Nthawi zonse mukakumbukire kuti muli pa nkondo ya uzimu ndimiyoyo ya amuna ndi akadzi.

Anthu amapereka zodandaula zomwe siziri za iwowo. Anavapo munthu akukamba ndiposo akuzengereza kuti athese nkhani yomwe imakambidwa pamenepo. Ena amabweresa zowiringula zomwe zikuwaphinja kuti asakapange chisankho chosata Yesu khirisitu. Zinthu izi ndizoyenera kuthana nazo, anthuwo asalandire Yesu.

Zowiringula kapena zodandaula ziri zonse zitha kuyakhidwa ndi Mawu a Mulungu. Musakalole zodandaula kuti zikazuse kwiyo kuti mukayambise mikangano. Izi zikachitika mumataya sogolo la kulalikira ndipo zowiringula zikakwanirisa zolinga zake.

Zotsala za phunziroli zakozedwa ndi malemba akuluakulu omwe akufotokoza mayankho osiyanasiyana amene mungalandire mukamagawa uthenga wabwino. Pamene mukuphunzira, kumbukirani zimene Mulungu amalankhula zokhuzana ndi zowiringula.

**Pakuti chilengedwere dziko lapansi zaoneka bwino zosaoneka zace ndizo mphamvu yace yosatha ndi umulungu wace; popeza zazindikirika ndi zinthu zolengedwa, kuti iwo adzakhale opanda mau akuwirungula. (Aroma 1:20)**

**“INE SIINE OYENERA”  
kapena  
“NDINE OCHIMWA KWAMBIRI”**

Anthu ena amazimva kuti siwoyenera kubwera pamaso pa Ambuye ndipo amafuna kudikira kufikira atazikodza okha.

Awoneseni kuti Mulungu amafuna chikhulupiriro osati kulimba kwa thupi. Yesu anabwera kudziko lapansi kuzapulumsa ochimwa osati olungama (Mateyu 9:12-13). Kusithika kwa kunja sikokwanira ngati mtima ukhalabe osasithika. Gwiritsani mavesi otsatirawa: Yesaya 1:18-19; Machitibwe 2:38; 1 Timoteo 1:15; 1 Yohane 1:7; Yohane 6:37; Cibvumbulutso 22:17; Aroma 5:8, 16, 20

**“MOYO WACHIKHRISTU NDIWOVUTA”**

Awoneseni kuti “Njira za munthu ochimwa ndizovuta” (Miyambo 13:15). Yesu amatipunzitsa kuti gori lake liri lofewa ndi katundu wake ali wo pepuka (Mateyu 11:28). Chisangalalo cha uchimo ndicha kanthawi kochepera koma zeni zeni ndi chimwemwe chamuyaya chichokera muchipulumutso (1 Petro 1:5 ndi Yuda 24).

**“SINDINGASIYE NJIRA ZANGA ZOYIPA”**

Vomerezanani nawo ndipo mugawane mau apa Aroma 7 amene amagwirizana ndi mfundo yawo. Kenako wonani ngati vuto lakelo ndiloti “siyingathe” kapena “siyizatha”. Afotokozereni kuti akakhala okhulupirira, atha kukhoza zonse mwa iye wawapatsa mphamvuyo (Afilipi 4:13). Awuzeni kuti tchimo ndi ukapolo ndipo njira imodzi yomwe angachokere muukapolo ndikuzera mu mwadzi wa Yesu (Yohane 8:24; Aroma 7-8)

**“MTIMA NDIWOUMA”**

Afunseni kuti ndikotheka kuti mtima wawo ungasithe, kodi angafune zitatero? Kenako gawanani mavesi awa Ezekieli 36:26-27 ndi Yohane 6:37

**“NDIZAKHALA NDI ANTHU AMBIRI KU GAHENA”**

Izi ndizoona, koma awonetseni mitundu yake ya anthu powerenga Chibvumbulutso 22:15. Awuzeni kuti kucheza ndi abwenzi kapena abale sikuzachepesa masautso opezeka pa Cibvumbulutso 20:10.

**“SINDINKHULUPIRIRA BAIBULO”  
kapena  
“SINDIRIVETSETSA BAIBULO”**

Afotokonzereni kuti palibe amene amavetsetsa zonse, koma mayankho amene Mulungu amafuna kuchipulumutso amavetsetseka mosavuta. Afotokozereni kuti pali zinthu zimene sangazivetsetse kufikira atakhala wonkhulupirira. (onani 1 Akorinto 2:14)

Onani ngati pali wina akuvuta kumvetsetsa Yohane 3:16; Macitidwe 16:31; 2:38; 3:19; Aroma 10:9-10; Machitidwe 22:16 and 6:1-4. Gwiritsani mavesi awa: Yohane 7:17; 1 Yohane 5:9-12; Marko 16:16; 2 Timoteo 3:16-17.

### **“MULI ZOTSUTSANA ZAMBIRI BAIBULO”**

Nthawi zina anthu akamva chowiringula ichi kwa anthu ena ndipo amangobwereza zomwe adamva zija. Afutseni kuti akuuzeni chotsutsana chimodzi. Nthawi zambiri munthu sanganene olo chimodzi. Ngati akuuzani chomwe akuganinza kuti chotsutsana, afotokozereni bwino bwino. Ngati simukuziwa yankho, kafufuzeni.

### **“NDIKUCHITA KWAKUNTHEKERA KWANGA”**

**kapena**

### **“NDILI OKODZEKA KALE”**

Izi zitha kukhala zoona potengera ndimachitidwe komanso zintchito zamunthu, koma sitinapulumsidwe potengera izi. Gwiritsani mavesi awa: Yesaya 64:6; Aefeso 2:8-9; Tito 3:5; 1 Yohane 1:7; Macitidwe 17:30; Afilipi 3:4-7; Aroma 2:1; 14:13

### **“ANTHU ANDINTCHINGIRA NJIRA”**

Munthu antha kugwiritsa ntchito kuti achibale kapena abwenzi atha kumamunena kapena kumutseka akankhala wokhulupirira. Werengani machenjezdo awa mu Luka 9:26; Aroma 14:12 ndi Macitidwe 5:29. Awuzeni kuti masautso amakhalapo (2 Timoteo 2:12; 3:12; 2 Akorinto 4:16, 18). Athanso kunena kuti akudikirira munthu wina, akhoza kukhala amuna awo kapena akadzi awo. Gwiritsani Mateyu 10:37. Atha kumawopa kutaya abale awo ochimwa akakhala okhulupirira. Gawanani Yakobo 4:4, Masalimo 1:1-2, ndi Miyambo 18:24.

### **“MULI ANTHU ONYENGA MU MPINGO”**

Vomerezanani nawo, Yesu ananena kale kuti zizakhala chocho (Mateyu 13:25, 47). Izi sizisintha zimene ananena Yesu paza moyo wake. Awonetseni kuti palibe onyenga ali yense akapezeka kumwamba (Cibvumbulutso 21:8). Mwina anapwetekedwapo mtima ndi okhulupirira ena. Akumbutseni kuti 1 Akorinto 2:5 limati chikhupiriro chanu cisakhale m'nzeru ya anthu koma mu mphamvu ya Mulungu. Akumbutseni kuti azayankha okha pa tsiku lachiwerunzo osati wina ayi. Gawanani 2:1-5 ndi Cibvumbulutso 20:12.

### **“SINDINGATHE KUSANKHA MPINGO OTI NDIROWE”**

**kapena**

### **“NDINE WACHIPEMBEDZO CHINA”**

Awunikireni kuti Baibulo siyimatiuza kulowa zipembezo zina koma kukhala mbali imodzi ya mpingo wachoonadi kudzera mukubadwatso mwatsopano. Musayitane aliyese kuti alowe chipembedzo chanu koma akaope Yesu ndikukhala thupi limodzi ndi khristu (Macitidwe 2:47). Akumbutseni kuti chipulumutso chiri mwa Yesu yekha osati kukhala membala wa mpingo (Macitidwe 4:12).

## **“NDACHEDWA”**

Kuwiringula uku kutha kuperekedwa ndi munthu amene akunzimva kuti iyeo ndi ochimwa kwambiri kapena munthu amene wakhala moyo wake onse muuchimo ndipo pano wakalamba. Akumbuseni kuti Mulungu safuna munthu aliyese kuti akatayike (2 Petro 3:9) ndiposo okuba uja pantanda anapulumsidwa munthawi yomaliza yamoyo wake (Luka 23:43).

## **“NSINDINGALANDIRE YESU KHRISTU PANOPA”**

Muwerengereni mavesi awa: Yesaya 55:6; Mateyu 24:44; Macitidwe 17:30; 22:16; 2 Akorinto 6:2; Yoswa 24:15; 1 Mafumu 18:21; Ahebri 2:3; Yakobo 4:13-24.

## **“MAVUTO ANGA NDIWOVUTA KWAMBIRI”**

Mulungu ndiye yankho kunyengo zovuta. Gawanani 2 Akorinto 12:9-10; Mateyu 19:26; Afilipi 4:13.

## **“NDANKHALA NDIKUFUNA KOMA SINDIPEZA”**

Anthu ena amati ankhala akufunafuna kukumana ndi Ambuye koma akanika kumupeza. Gawanani mavesi awa: Yeremiya 19:13; Luka 19:10; Yohane 1:12.

## **“MULUNGU NDIWOYENERA KUNDIRANGA”**

Gawanani: Aroma 2:4-5; 2 Petro 3:9-11; Ezekieli 33:11.

## **“SINDINGATHE KUNKHULULUKIRA WINA”**

Anthu amagwirisa ntchito kuwiringula uku koti sangathe kunkhulukira wina amene adawalakwirapo, ndiye sangapulumsidwe. Izi zintha kukhala zoonza kwa munthu amene maganizo ake sanasithidwe, koma ngati akhristu, Mulungu atha kutithandiza kuti tipange izi. Gawanani Marko 11:25 ndi Yakobo 4:6.

## **“NDIZOSATHEKA NDI NTCHITO YANGA”**

Anthu ena amapereka kuwiringula uku chifukwa amaganiza kuti asiya ntchito yawo ndikulowa mu utimiki. Awuzeni kuti tsiziri chocho. Afunseni kuti akugwira ntchito yanji. Ngati ntchito yawo siyikugwirizana ndimalamulo achi khristu, awuzeni kuti koyenera kuti asiye ntchito. Chifukwa ndikoyenera kutero kuposa kukataya moyo wawo ku gahena. Gawanani Marko 8:36.

## **“NDINAYESAPO KOMA NDINALEPHERA”**

**kapena**

## **“NDIKUWOPA KUTI NDIREPHERA”**

Ayamikireni chifukwa choskhala omasuka kukamba zakulephera kwawo, koma awonetsereni kuti Mulungu walonjedza zamphamvu zothandizira kuthana ndi tchimo. Gawanani mavesi awa Aroma 8:37; 1 Akorinto 10:13; 1 Petro 1:5; 2 Timoteo 1:12 ndi Ahebri 13:5.



Ganizani zifukwa zimene akuganizira kuti alephera. Anayeserapo kudalira Mulungu? Anawadziwa machimo awo asanawalape? Anapita njira ya dziko kusiya ku Mau a Mulungu? Anawerenga Baibulo, kupephera ndikupita ku kachisi mowirikidza?

Apaseni chiyembekedzo ndi kuwalimbitsa mtima kuti akachitenso. Akumbutseni kuti zifundo za Mulungu zimakozedwa tsiku ndi tsiku ndipo sizirephera (Maliro 3:21-24). Gawanani 2 Akorinto 9:8; 12:9; 1 Yohane 1:9; Yuda 24; 2 Timoteo 1:12; 1 Peter 1:5. Ndikukhulupirira osati kuyesera komwe kumabwera chipulumutso. Gawanani Yohane 1:12 ndi Aroma 4:3-5.

### **“NDIRIBE KUTSIMIKIDZIKA MTIMA”**

Nthawi zina ukamutsogolera munthu Kwa Ambuye amatha kukhala osasimikidzika mtima za chipulumutso. Awuze kuti akana kukhulupirira kuti Mau a Mulungu nd tchimo (Aroma 14:23). Gawanani mavesi awa amene amanena zaku tsimikizika mu chipulumutso: Yohane 1:12; 3:16, 18, 36; 5:24; Machitidwe 10:43; 13:39; Aefeso 1:17-20; 2:8; Yuda 24, 2 Timoteo 1:12; 1 Petro 1:5, 18-19; 1 Yohane 1:7; 5:13; Ahebri 9:22-10:22; 2 Akorinto 5:17; Aroma 5:1,9; 3:25; 8:16.

### **“KUKANIDWA KWANANU”**

Werengani Luka 10:10-12. Pamene mukulalikira ndipo Uthenga Wabwino wanu wakanidwa kwananu, mukuyenera kuchoka ndikupita kwa munthu wina kapena dera lomwe lingalandire uthengawo.

## MAFUTSO OZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera

---

---

2. Chifukwa chiyani anthu amawirungula pochita uvangeli?

---

---

3. Kodi mungathane bwanji ndimavuto omwe amachitikachitika pa uvangeli? Lembani mayakho anu pa pepala yina

- “Siine oyenera”
- “Moyo wachi khristu ndiwovuta”
- “sindingasiye njira zanga zoyipa”
- “Mtima wanga ndiwoyipa”
- “Ndizakhala ndi azanga ambiri ku Gehena”
- “Sindikholupirira Baibulo”
- “Muli zotsutsana zambiri Baibulo”
- “Ndikuchita mwakuthekera kwanga”
- “Anthu ena ayima panjira yanga”
- “Muli onyenga ambiri mu mpingo”
- “Ndine wachipembedzo china”
- “Ndachedwa”
- “Sindingalandire Yesu Pano”
- “Mavuto anga ndiwovuta zedi”
- “Ndakhala ndikufuna koma sindipedza”
- “Mulungi ndiwoyenera kundiranga”
- “Sindingakwanitse kukukhulukira wina”
- “Sindingakwanitse chifukwa cha ntchito yanga”
- “Ndinayeserapo koma ndinalaphera”
- “Ndilibe kunsimikidza mtima”

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

## ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Izi ndi zinthu zina zomwe mukuyenera kukumbukira pothana ndimavuto omwe mukukumana nawo potumikira:

1. Kumbukirani kuti mukuthana ndi nkhondo ya uzimu kumuyoyo ya amuna ndi akadzi. Muzamenye khondo yawuzimu ndi zida zaku nthupi monga kusutsana ndiku kwiya.
2. Musathese ganizo ngati kuti ndilopanda ntchito. Litha kukhala lofunika kwamunthuyo.
3. Musakhalitse pa kuwirungula. Munthane nazo mwachangu, modekha komanso mwanzero, kenako bwererani ku fundo zomwe mumakamba zowamangilira kwa Ambuye.
4. Musakangane
5. Musakwiye
6. Mukhale amzeru komanso afundo
7. Dalirani mzimu waMulungu komanso Mawu aMulungu
8. Pitirizani kubwerera kufundo zanu
9. Musanyodze
10. Mutsanyodzetse
11. Musataye mtima ndikusiya panjira

## CHAPUTALA 11

### NJIRA: UVANGELI WOCHULUKITSA

#### ZOLINGA:

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba mavesi otsogolera
- Kufotokoza kuti “uvangeli ochululitsa ndichani”
- Kulemba mwachidule maziko a Baibulo a uvangeli wochulukitsa
- Kakamba zoyenera kusatira mu uvangeli wochulukitsa
- Kukamba mmene umakhalira uvangeli wochulukitsa
- Kufotokoza momwe abusa angakozesekere mpingo wawo ku uvangeli wochulukitsa.

#### VESI YOTSOGOLERA:

**Mu mphamvu ya zizindikilo ndi zozizwitsa, mu mphamvu ya Mzimu Woyera; kotero kuti ine kuyambira ku Yerusakemu ndi kuzungulirako kufikira ku Iluriko, ndinakwanitsa Uthenga Wabwino wa kristu; (Aroma 15:19)**

#### CHIYAMBI

Mawu oti “chulukitsa” akutanthauza kuti “kukwaniritsa ndichinthu choti chimalowerera ponseponse”. Uvangeli wochulukitsa ndi njira yofalitsira Uthenga Wabwino omwe umagwira ntchito mofafanana ndi chotupitsa mu mkate. Cholinga chake ndikufalitsa Uthenga Wabwino kufikira dera lonse litafikiridwa paliponse. Kuyambira ku dera lomwe mumakhala (Yerusalemu wanu), uvangeli wochulukitsa umafalikira kufikira mu dera lanu kapena chigawo ndi pamapeto pake dziko lanu.

#### ZIMENE BAIBULO LIMANENA ZA UVANGELI WOCHULUKITSA

Mawu oti “uvangeli wochulukitsa” samapedzeka m’Baibulo, komanso mawu oti uvangeli, uvangeli wa panokh uvangeli wakwa gulu. Chipangano chatsopano chimakamba zambiri za ntchito za uvangeli ngakhale mawu eni eni sagwiritsidwa ntchito.

Komabe, uvangeli wochulukitsa unafotokozeredwa bwino mu Chipangano chatsopano. Akulu akulu adanena kuti atumwi adzaza Yerusalemu ndi ciphunzitso canu (Machitidwe 5:28). Mpingo wa m’Yudeya, Galileya ndi Samariya unali olimbikitsidwa. Onse okhala mu Lidiya ndi ku Sarona anatembenukira kwa Ambuye ndipo Jopa anadziwitsidwa za Uthenga Wabwino (Macitidwe 9:31, 35, 42). Zikwi zikwi za Ayuda zinatembenukira kwa Ambuye (Macitidwe 21:20). Ku Antiokekeya wa m’Pisidiya komanso ku Korinto kudaveka “Ndipo mau a Ambuye anabukitsidwa m’dziko lonse” (Macitidwe 13:49).

Kotero kuti onse akukhala m’Asiya anamva Mau a Mulungu (Macitidwe 19:10), mwina kufotokoza kwakukulu kwa uvangeli wochulukitsa kunachokera mu makalata a Paulo:

**Mu mphamvu ya zizindikilo ndi zozizwitsa, mu mphamvu ya Mzimu Woyera; kotero kuti ine kuyambira ku Yerusalemu ndi kuzungulirako kufikira ku Iluriko, ndinakwanitsa Uthenga Wabwino wa Kristu.**

**Ndipo coteru ndinaciyesa cinthu caulemu kulalikira Uthenga Wabwino, pa malopo Kristu asanachulidwe kale, kuti ndisamange nyumba pa maziko a munthu wina.**

**Koma monga kwalembedwa, Iwo amene uthenga wace sunawafikire, azaona, ndipo iwo amene sanamve adzadziwitsa. (Aroma 15:19-21)**

## **MFUNDO ZIKULUZIKULU ZA UVANGELI WOCHULUKITSA**

Uvangeli wochulukitsa unakhazikisidwa pa mfundo izi:

### **KUFETSA MOLOWA MANJA, MOLOWA MANJASO ADZATUTA**

Mtumwi Paulo akuwuzza mpingo waku Akorinto:

**Koma nditi ici, kuti iye wakufesa mouma manja, mouma manjanso adzatuta. Ndipo iye wakufesa moolowa manja, moolowa manjanso adzatuta. (2 Akorinto 9:6).**

Zayikidwa ku uvangeli, lamulo la zokolola ili likutathaunza kuti ndi mpingo okhawo omwe umagwira ntchito ya uvangeli ndi umune ukakolole miyoyo ya anthu ambiri. Ziribe kanthu kuti mbewu ndiyabwino bwanji, nthaka ndiyachonde bwanji kapena kuti mulimi ali ndi lutha lanji, sangakolole opanda kufesa. Abusa ndi mpingo omwe safesa mu uvangeli sangathe kuona zotsatira za uvangeli. Uvangeli wochulukitsa umafuna nthawi, anthu, kulimbikira, pemphero, misozi, ndi chuma chothandizira uvangeli.

### **ANTHU OZIPEREKA OCHEPA ANTHA KUSINTHA DZIKO:**

Baibulo limatiwonesa kuti Mulungu safuna kugwira ntchito ndi anthu ambiri koma anthu ochepa. Kumbukirani kuti Mulungu adabwedza asirikali akhondo a Gideyoni ndikugwiritsa ntchito asilikali okwana 300. Zimatengera anthu ochepa omwe ali odzazidwa ndi Mzimu Woyera kukasintha dziko lonse (Macitidwe 17:6), umu ndimomweso zikuchitikira matsiku ano.

Ngakhale okhulupirira atasonkhanitsidwa ku uvangeli, m'zinda ndi kumayiko, azakhalabe ochepa malingana ndi mmene ntundu wa anthu uliri ochuluka. Koma izi sizilepheresa uvangeli wochulukitsa. Pamene Mulungu wachita zazikulu kudzera kwa anthu ochepa, Ulemerero umapita kwa iyeo osati kwa munthu.

### **OKHULUPIRIRA ALIYENSE AKUYENERA ATSONKHANITSIDWE:**

Uvangeli wochulukitsa umafuna kuti okhulupirira alimbikitsidwe komanso atsonkhanitsidwe ku ntchito ya uvangeli. Kutsonkhanitsa kumatengera ndimene wayimira muwubale ndi Mulungu wako, kulimbikitsidwa ndi chikumbu mtima ku dziko lomwe latayika komanso lomwe likufa. Zimafunanso ubale oyima njii kwa wina ndi mzake. Pamene Mulungu akukuyendesa ndi Mzimu Wake, chikhumbokhumbo chako chimafalikira ndikukhudzanso anthu ena.

Zomwe anthu amaziwa ndi zoti utimiki unayikizidwa mwa abusa basi. Mu uvanvangeli wochulukitsa, ukukamba zakusintha kuchokera pagome kupita kwa anthu. Koma si utumiki umene umawapatula abusa, iwowo ntchito yawo ngati mtsogoleri ndi wofunika kwambiri. Ndiwo amene ali woyenera kutsonkhanitsa mpingo wawo.

Kutsonkhanitsa mpingo ku uvangeli kukuyenera kuchitika potengera mphatso za umzimu, membala aliyense agwire ntchito mu dera lomwe likugwirizana ndi mphatso zake. (The Harvestime International Institute course “Njira Zotsonkhanitsira” ikufotokoza mwa tsatanetsatane za kutsonkhanitsa.)

### **KUTSONKHANITSA PA NTCHITO YOMWE IMACHITIKA PA MPINGO:**

Mu uvangeli wochulukitsa tikamalankhula za mpingo, timakhala tikutanthauza mpingo wam’dera lanu, gulu la mipingo, ndi Mpingo omwe uli okhulupirira onse a dziko lapansi.

Uvangeli wochulukitsa umayenera kukhudza mpingo wa m’dera lanu komanso kufikira zipembedzo zonse. Ngati mpingo uli onse m’dera komanso zipembedzo dzina zingazipereke ku uvangeli okuya ngati uwu, izi zitha kupereka zotsatira zabwino zotsonkhanitsa a khristu onse kunkhala okhulupirira eni eni. Chimango cha kutsonkhanitsa ndi kukhudzidwa kuti Mpingo ndi njira imene Mulungu waisankha kuti ionetsere zinsinsi za Uthenga Wabwino ku dziko lonse lapansi (Aefeso 3:9-10).

### **TAKHANZIKIKA PAKUTI “PITANI” KUPOSA PAKUTI “BWERANI”:**

Munthawi ya tsopano ino mipingo yambiri inatenga kwambiri mawu oti “bwerani” ngati njira ya uvangeli. Amatsegula zitseko za mipingo yawo nthawi ya uthenga ndipo amadikirira kuti anthu osapuluma abwera. Koma Chipangano Chatsopano chikutiphunzitsa kuti “tipite”. Mpingo ukuyenera kupita kudziko lapansi ndi Uthenga Wabwino. Uvangeli wochulukitsa umafunikira kuti anthu achonse muma kachisi awo ndikupita ku dziko.

### **UMODZI MUUMZIMU NDIKOFUNIKIRA**

Uvangeli wochulukitsa umafunikira umbozi wogwirizana pakati okhulupirira ndi anthu azipembedzo dzina. Umboni uwu siutsutsa Ochikumbu mtima chawina kapena chipembedzo china. Pakutin mwa mzimu mmodzi tinayenerezedwa ndi Mzimu wa Mulungu (1 Akorinto 12:13). Mizimu yanthu ili yogwirizana kuntchito ya uvangeli.

Anthu a Mulungu amatchedwa thupi la Kristu (Aefeso 4:12). Ngat ziri zoon, tikachitechite ngati a nthupi limodzi osati ngati siife athupi limodzi. (Mukaphunzira kwambiri za izi pamene muzikaphudzira za utumika wogwirizana mu Mutu Khumi ndi Chisano.) Uvangeli wochulukitsa umayesera kupeza mipingo, mautumiki, zipembedzo komanso mabungwe othechera kuti akakwaniritse uvangeli.

### **NDIWA DZIKO LONSE:**

Utumiki waukulu unaperekedwa kwa ophunzira ake onse a Khristu komanso lamulo linaperekedwa kwa zolengedwa zonse. Uvangeli wochulukitsa umagwiritsa ntchito njira iri yonse yovemerezeka yomwe yapezekayo kupereka uthenga kwa anthu onse komanso popereka Uthenga Wabwino kwa mitundu yonse.

Munyengo zambiri, zolinga zauvangeli zimakhala zofooka. Timakhala ndimaganinzo okafikira kumadera ang’ono ang’ono okha. Kugwira ntchito ndi ndalama zochepa komanso

masopenya ochepa, nthawi zina timakhulupirira kuti takwaniritsa ntchito yathu pamene tagwira ntchito Madera ochepa amuzinda kapena ku dziko.

Pamene Kristu anatilamula kuti tipite ndi kukaphunzisa mitundu amatanthauza kuti tikafikire mitundu yonse. Uvangeli wochulukitsawu uli wa dziko lonse, mitundu yonse ikafikiridwa ndiye kuti dziko lonse lifikiridwa.

### **NDONDOMEKO YA UVANGELI WOCHULUKITSA**

Uvangeli wochulukitsa umatenga ndondomeko zosiyanasiyana zogwirira ntchito ku dziko lonse. Zinkhalidwe zadziko chimasiyana ndiposo ndizachiziwikire kuti uvaneli umagwiritsa ndondomeko zosiyanasiyana. Tikuyenera kudziwa njira yoyenera komanso ya mphamvu imene siyingakhale yamphamvu ndi yoyenera muchikhalidwe china.

Ndondomeko zoyenera mu uvangeli wochulukitsa, nthawi zina, mumayenera kulemba mmene mungafikire kwa mitundu ya anthu a mitundu yonse, komanso, mayiko onse a dziko lapansi. Mumsimu muli ndondomeko zoyenera mu kulalikira wochulukitsa: stapler

#### **BUNGWE:**

Kuti mitundu yonse ikafikiridwe, pakuyenera kukhala kulumikizana bwino pakati pa ntchito yonse ya uvangeli. Kukwaniritsa ichi, koyenera kuti komiti lotsogolera uvangeli likhazikitsidwe mu mpingo uli onse. Komiti imeneri ikakhala lokhudzidwa ndu uvangeli wa mdera lomwe liri komanso kufikira anthu onse a m'deralo.

Komiti ya mzinda ikuyenera kukhazikitsidwa ndi mipingo ya mu dera kuti ukayang'anire uvangeli wa muzindawo. Ichi chikathandizira kupereka gwirizano osati pikitsano pakati pa mipindo yama dera. Komiti ya chigawo ikhala yokhudzidwa ndi chigawo chonse, ndi komiti ya dziko lonse yomwe iziona uvangeli wa dziko lonse.

Makomiti azisiyana mmalinga ndi chochitika ndi zolinga za mzinda, chigawo, ndi mdziko. Koma komiti iriyonse itha kukhala ndi mamembala awa:

-Wapampando: Otsogolera komanso kuyendetsa gulu

-Otsara kwa wapampando: Othandiza wapampando komanso mlowa malo ngati iye palibe.

Mlembi: Azigwira ntchito za ukalaliki ngati makalata, kulemba pa mkumano, kusunga zolemba ndi zina zambiri

-msungi mchuma: Azisunga chuma, ndondomeko ya kagwiritsidwe ka chuma

-nkulu oyendetsa mapephero: Azitsogolera mapephero okonzekera ntchito ya uvangeli.

-oyendesa ziphunzitso: Amene aziringaniza maphunziro a uvangeli.

-Ofalitsa uthena: ofalitsa uthenga mapologalamu a utumiki pa wailesi, kaname yowulusa mawu, mkhuni, mumagalimoto, zinthuzi komaso kutumiza mauthenga.

#### **ZOYENERA KUCHITA:**

Pakuyenera kukhala dongosolo lazoyenera kuchitika mu uvangeli wochulukitsa. Umu ndi momwe mungapangire dongosolo lanu lazochitika pa chaka:

January: kumanani ndi atsogoleri amipingo yonse,  
kuyambira Madera, mizinda komanso a dziko lonse.

February: Phunzitsani atsogoleri onse.

March: Phunzitsani a khristu onse.

April: } Kuchulukitsa madera ang'ono ang'ono  
May: } } kudzera njira zosiyanasiyana za  
June: } uvangeli

July: kulalikira m'madera ang'onoango

August: kuyendera madera ang'ono ang'ono

September: Kulalikira madera a mzigawo

October: kuyendera anthu a mzigawo

November: Kulalikira dziko lonse

December: kuyendera anthu ndi kupanga dongosolo ya chaka chotsatira

(Mu Chaputala 12 muphunzira mmene mungachitire komanso kupangira chitsitsimutso. Mu Chaputala 13 mukaphunzira mmene mungalondolere anthu omwe alandira Yesu kumene komanso kuwaphunzitsa mene angakhalire ophunzira a Yesu.)

### **NJIRA:**

Pa mtundu uli wonse wa uvangeli omwe umagwiritsidwa ku amdera ang'onoang'ono, muzigawo ndi pa dziko lonse, muzipanga zotsatirazi:

- Kukumana kupepherera uvangeli
- uvangeli wapa wailesi ndi pakanema.
- Kukhala ndi uthenga muma kaseti
- Kuonesa kanema
- Kugawana mawu amu m'Baibulo kunyumba, mu kachisi, kumadera okumaniranako.
- Maphunziro a uvangeli.
- Kumema anthu kuti abwere ku kachisi kapena ku mitsonkhano kuchitsitsimutso
- Kulalikira nkomo ndi nkondo
- Kulalikira asilikali
- Kulalikira anthu amalonda ndi zintchito
- Kuphunzitsa anthu za kulalikira
- Kubweretsa njira za chipatala koma mukulalikirara kwa anthu Uthenga Wabwino
- kuwayimbira ma phone anthu.



- Kuyenda yenda pagalimoto kuwauza anthu za Uthenga wabwino komanso kuwayitana kuti abwere kuchitsitsimutso.
- Kuwalemba kalata yogawana nawo Uthenga Wabwino
- Kupita ku ndende, zipatala komanso manyumba mwa anthu otayika.
- Tumikirani ku ma sukulu amipingo: ku sande sukulu, ma sukulu aza Baibulo komanso ku ukachenjede waza Baibulo.
- Lalikirani mu malo ochedzera, mu msika ndi malo omwe anthu ambiri amakumana.
- Tumikirani momwe akupanga mikumana yapaderadera, monga ngati maukwati, komwe anthu amawonerako masewero kapena patsokhano wachipani.
- Pangani ziwonesero zosiyana siyana ngati kuyimba, ndakatulo komanso kupanga sewero.
- Gwiritsani mabuku: gawani mathilakiti, ma buku ndi zinthu zina sozindikizidwa.
- Tumikirani kumagulu adzotsowa zapaderadera: amowa, amankhwala, anjala, osowa pogona, mosamalira ana, osokonezeka maganizo komanso muthupi mwawo.
- Gawani kulalikira wanu kufikira ana, achinyamata, abambo komanso azimayi.
- Katumikireni ophunzira omwe ali ochokera kunja amene akuphunzira sukulu zaukachenjede madera anu.
- Katumikireni ma sukulu.
- Pangani zitsitsimutso zamu dera, midzinda komanso dzamu dziko.

Zina mwa njira zomwe zalembedwa mwambamo sizingatheke mumayiko ena chifukwa chamalamulo awo a dziko. Koma mfundo ndiyoti uvangeli wochulukitsa umafuna khama pofujna kufikira dziko lonse ndi Uthenga Wabwino munjira yomwe iri yoyenera.

Palibe malire ku njira zomwe zingayikidwe ku uvangeli wochulukitsa. Kumbukirani kuti cholinga ndikufikira aliyense ndi Uthenga wabwino.

### **KUKODZEKERETSA MPINGO WA M'DERA LANU**

Chifukwa chonena kuti ntchito m'zigawo ndi dziko lonse imaphukira kuchoker m'madera ang'ono ang'ono, komanso chifukwa choti uvangeli wochulukitsa umachita kwambiri mipingo yama dera, ndichofunikira kwambiri kwa m'busa kuziwa mmene angakozekeretsere mpingo wake ku uvangeli wochulukitsa. Izi ndi njira zomwe m'busa angakwaniritsire zolingazo:

- Inuyo khalani chitsanzo: Mpingo wanu ukaona kuti muli okondwa ndi uvangeli ndi kupulumusa miyoyo, uzakhuzika ndi changu chanu.
- Lunjikani uthenga wa chipembedzo cha m'mawa pa tsiku la Sabata kwa anthu osapulumsidwa. Ngati anthu osapulumuka amabwera ku kachisi, amabwera nthawi zambiri mammawa.
- Nthawi ndi nthawi, muzilalikira uthenga wa uvangeli.

-Pangani mauthenga anu akhale muma kaseti: izi zikhoza kukhala uthenga owonera kapena overa mukaseti, mafilimu komanso bukhu lomwe lagona paza uvangeli.

-Pangani kuti atsogoleri ampingo wanu athe kumawina miyoyo. Chomuyeneredza tsogoleri aliyese chikhale choti akutha kuwina miyoyo. Ngati atsogoleri anu sakukwanitsa kuwina miyoyo kwa Ambuye, yambani kuwaphunizitsa.

-Sukulu ya Sabata maphunziro ake azilunjika pa kuwina wimyoyo: Aphunizitsi aphunzitsidwe mene akaperekere Uthenga Wabwino ndi kuwalola ana kuti awulandire. Makolo awo a ana omwe sanatembenuke mtima afikiridwe.

-Pangani kuti cholinga chamikumano yanu ikhale yokambirana za uvangeli: Mikumano yambiri matsiku ano yakhala yomangoyimba nyimbo, kukalikira bwino koma kupemphera kwenikweni kochepa. Atsogolereni anthu anu ku kupemphera kwakale komwe kumatsogozedwa ndi Mzimu Woyera, Kupemphera kwa Chipangano chatsopano kokhala ndicholinga kwa iwo otayikamo komanso kuzusa ziphona zogwira ntchito ya Mulungu.

-Chititsani mowirikidza ziphunzitso za uvangeli: mutha kugwiritsa ntchiito phunzirori la “Chotupitsa-ngati uvangeli,” ndicholinga chimenecho. Pitirizani kubwereza kalasi pomwe anthu atsopano abwera ku kachisi kapena ngati anthu ena alandira Ambuye.

-Pangani dongosolo la dera lanu: pezani mapu a dera kapena dzinda wanu. Gawani magawo angapo ndipo muyike atsogoleri mugawo liri lonse. Kenako....

-Ikidzani tsiku limodzi pasabata lopanga uvangeli. Timapanga zinthu zomwe tazipasa nthawi kuti tichite, uwu ndiye uvangeli weni weni. Simungawine miyoyo ngati simunapatule nthawi kuti muchiti.

-Patulani tsiku ndi nthawi, kumanani ndiwogwira ntchito, kenako atumeni awiri awiri. Apaseni ntchito yoti akayendere mabanja, malonda, mitsika ing’onoing’sono, mitsika ikulu ikulu, kogulitsira mafuta agalimoto, komwera mowa, atumizeni palipose umenewu ndiwo uvangeli ochulukitsa.

-Khazikisani pologalamu yoilondoloza anthu omwe munakawalalikira: Aphunzitseni anthu anu kuti akhale ndi udindo wama londoloza anthu omwe atembenku mitima. Yambani kalasi yatsopano yophunzitsa za chikhulupiro chachi khristu ndi kuwauza kuti azibwera ku kachisi.

## MAFUNSO OZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera.

---

---

---

2. Tanthauzirani “uvangeli wochulukitsa.”

---

---

---

3. Fotokozani zomwe Baibulo limakamba za uvangeli wochulukitsa.

---

---

---

4. Fotokozani ndondomeko ya uvangeli wochulukitsa.

---

---

---

5. Fotokozani ndongosolo a uvangel wochulukitsa.

---

---

---

6. Fotokozani mmene m’busa wadera angakozekeretsere mpingo wake ku uvangeli wochulukitsa.

---

---

---

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

## ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. The Harvestime International Institute course “*Kusanthula Zachirengedwe*,” ikufotokoza mmene munganthulire mudzi, dzinda kapena dziko kuti Uthenga wabwino ukafikire paliponse. Zikuthandizirani mmene mungaziwire zofunikira ndikugwiritsa dongosolo lanu ku kulalikirira wochulukitsa.
2. Pangani dongosolo ya uvangeli wochulukitsa mu mzinda kapena mudzi omwe mumakhala. Pepherani zokhudza kulalikirira zomwe mukufuna zikachitike kenako pangani ndondomeko yamomwe zitayendere malingaliro anu. Ndi mipingo kapena mabungwe achikristu anji omwe angakuthandizireni kufalitsa Uthenga mudera lanu?
3. Ngati mukuphunziro phunzirori muli ku ndende, pangani dongosolo la uvangeli wochulukitsa za malo omwe inu muliko. Ngati ndende yanu kuli m’busa, afuseni akuthandizeni.

## CHAPUTALA 12

### NJIRA: MTSONKHANO WA UVANGELI

#### ZOLINGA:

- Kulemba vesi yotsogolera.
- Fotokozani ubwino wa mtsonkhano wa uvangeli.
- Kulemba mwachidule nkhani zomwe zakambidwa mu phunziroli zokhuza:
  - Kukodzekera mu uzimu
  - Dera lopangira Chitsitsimutso
  - Malo ogwirira ntchito
  - Tsiku ndi nthawi
  - Kulengeza za mtsonkhano
  - Za chuma
  - Kukonzekera nthawi isanfike
  - Kuphunzitsa ogwira ntchito
  - Kuchititsa misonkhano
  - Kulondoloza
- Kuchititsa Chitsitsimutso chachikulu.

#### VESI YOTSOGOLERA:

**Penyani mwa amitundu, penyetsetsani, nimudabwe kwakukuru, pakuti ndicita ntchito masiku anu, imene simudzavomera cinkana akufotokozerani. (Habakuku 1:5)**

#### CHIYAMBI

Kumadera, m'zinda kapena mudziko Uthenga Wabwino sungafalikire popando mitsonkhano yayikulu. Pali nkhamu la anthu loyenera kuti likafikiridwe ndi Uthenga Wabwino, ndipo mitsokhano yayikuluyi imakhazikika kwambiri ofikira nkhamu la anthu kwa nthawi imodzi.

Pa Mutu Wachisano ndi Chiwire mwaphunzira kuchita uvangeli wa kwa munthu modzi modzi. Phunziro iri likufotokoza mene mungapangire misokhano ikulu ikulu. Zonse zinagwiritsidwa ntchito mu Chipangano Chatsopano, ndiponso zonse zikadali zofunikira mu uvangeli wamasiku ano.

#### MITSONKHANO IKULUIKULU YA UVANGELI

Njira imodzi yopangira uvangeli wa gulu ndikupanga mitsonkhano ikuluikulu chomwe umabweresa ntchito imodzi kwa okhulupirira kuti akafikire kwa wina aliyese mudera ndi Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu.

Iyi simikumano yomwe imangochitika magawo odzungulira kachisi. Si chitsitsimutso, chitsitsimutso chimakamba zobweresa chinthu chomwe chinali chamoyo koma chikupita kwakufa. Chitsitsimutso ndichakwa okhulupirira okha okha amene adzirala muuzimuu. Msokhano waukulu wa uvangeli umachitika kuti mukafikire mtundu wa anthu omwe sunatembenuke mtima mu dera lonse.

Mtsonkhano wa ukulu wa uvangeli umagwiridzana ndi malemba a m'Baibulo. Mwachinsanzo mu chipango chatsopano timawerenga kuti Yesu Khristu anayankhula ku khamu la anthu lokwana pafupifupi 150. Paulo ndi ophunzira ena amatumikira misika momwe anthu ambiri amakumana.

Tsonkhana waukulu umafikira anthu amene akhala akufunafuna Mulungu kwa nthawi yayitali. Umafikira anthu amene sanapiteko ku kachisi. Umapereka mwayi owonetsera mphamvu ya Mulungu kwa anthu osakhulupirira. Umapangitsa kuti Uthenga Wabwino ufikire kwa anthu mwachangu komanso ndinjira yofunikira kwambiri yofikira mitundu ya anthu ambiri ku dziko.

Mtsonkhano wa uvangeli umakunthandizirani kuti mukaziwe ngati pamalopo pali chonde chawuzimu kuti mungakolole anthu komanso ngati malowo ali wokozeza kukankhazikitsa mpingo. Ngati pamalopo pali kale mipingo ina, kukula kumachitika pamene anthu ena alandira Uthenga Wabwino amalowa mipingo yawoyo.

### **KUZI-KODZEKERETSA MU UMZIMU**

Maganizo amu phunziro iri akhazikitsidwa pofuna kukutsogolererani mmene mungachitire pofuna kupanga mtsonkhano wa uvangeli. Koma mukuyenera kudziwa kuti mukangozikonzekeretsa kuthupi popanda mphamvu ya uzimu, mukakhala ngati “mungoyakhula popanda chirichonse chotsatira.” Kudzikonzekeretsa mu uzimu ndichinthu chofunika kwambiri mu kulalikira.

Musalole kuti mukagwe mumayetsero otanganika ndintchito zozikonzekeretsa kuthupi kusiya kukodzekera bwino bwino mu uzimu wanu. Mtsonkhano umakhala wamphamvu pamene Uthenga wa Ufumu wa Mulungu waperekedwa ndikudzodza komanso ndi Mphamvu ya Mzimu Woyera yomwe imapulumutsa, kuchiritsa komanso kumatsula ndipo izi zimafunikira kukodzekera kwambiri mu Uzimu.

### **DERA LOPANGIRAKO CHITSITSIMUTSO**

Cholinga cha chitsitsimutso chachikulu ndikubweresa Uthenga Wabwino kwa amene sanawuvepo. Kumene mukapangire msonkhano kukhoza kutsimikizidwa mu imodz mwa njira izi:

**Choyamba:** mutha kulandira kuyatanidwa kuchokera kwa abusa, a mishoni kapenanso okhulupirira ochokera dera lina kuti mupite mukachititse msonkhano. Pepherani kaye musanavomere ndipo ngati mwakhulupirira kuti zikuchokera kwa Mulungu, mutha kuvomera.

**Chachiwiri:** mutha kutsogozedwa ndi Mulungu kupita dera lina. Pa ichi, mutha kulumikizana ndi okhulupirira aku dera lomwe mukupitako ndikuwauza chapa mtima panu ndiposo kuti mukathe kugwiridzana ngati kuli kotheka. Ngati kulibeko okhulupirira ngakhaleso mipingo yokhazikika mu deralo, kapena simunathe kugwiridzana, mukuyenerabe kupita ngati mukukhulupirira kuti Mulungu ndiyemwe wakutumani.

Ngati uli msonkhano wa dziko lonse, mzinda wawukulu wa dziko kapena mzinda wina okulirapo ndiwomwe ukuyenera kusakhidwa. Mzinda ukasakhidwa, kenaka malo ochitira msonkhano mzindawo asankhidwensho. Ichi chofunikira kwambiri, chifukwa muntha kupanga

chiri chonse bwino bwino koma ngati anthu sakwanitsa kufika kumaloko, ndiye kuti kulimbikira kwanu konse sikungawoneke. Malo abwino ochitira msokhano wanu akhale oyandikana kwambiri ndikumalo komwe kumakhala anthu ambiri.

Awa ndi malo amene mungapangire msonkhano:

### **MALO POMWE PALI PANTETETE KOMA AKULU**

Kwa nthawi yayitali malo awa awonesa kuti ndi abwino kuchitira msonkhano. Muntha kupanga gome lanu pamalopo ndiposo anthu ambiri antha kufikira pamalopa. Muthaso kugwirisa ndalama zochepa.

### **MALO OMWE ANTHU AMACHEZERA:**

Muyenera kukapepha chiroledzo kwa akulu akulu oyang'anira mzinda kuti mugwirisira ntchito malo amenewa. Ubwino wa malo amenewa ndiwoti malowa ndiwoziwika kwa anthu amuderali komanso anthu ambiri amabwerabwera kumalowa komanso iwo amane sabwera anthaso kubwera. Munthaso kugwiritsa ntchito malowa kwa ulere kapena ndi ndalama yochepa.

### **MALO OCHITIRA MASEWERO:**

Malo ochitira masewero ndimalo odziwika kwambiri ndi anthu onse amzindawo. Mukhale otsamalitsa pokatenga chiroledza chogwiritsa ntchito malo ochitira masewero ndiposo muone mene mungazamangire gome lanu. Malo amasewero abwino amayitananso anthu ochuluka. Muyendere makomo onse olowera komanso otulukira kuti ali bwino komanso ndiwokwanira.

(Onetsetsani kuti: Musagwiritse ntchito zinthu za mpingo chifukwa zimaphinja kufikira anthu ena. Anthu ambiri omwe sanapululumuke samamva bwino kupita ku kachisi. Zipembedzo zina zimalesa ma membala awo kupita ku mipingo ina.)

Malo onse muntha kuwonjedzeramo izi:

- Malo okhala
- Malo akulu oyimitsira magalimoto
- Malo ambiri olowera ndikutulukira
- Kukhale kufipi ndikokwerera mabasi
- Kukhaleso magetsi owunikira ndi zoyimbira
- Kukhaleso zimbuzi

### **MGWIRIZANO WA MALO**

Mukuyenera kusayinirana pamgwirizano okhuzana malo musanayambe kulengedzetsa za malo opangira msonkhano. Zina mwazomwe mutha kugwirizana:

1. Dzina lanu komanso lamunthuyo, dzina la bungwe lomwe likukubwerekani malowo
2. Matsiku eni eni mutagwiritsire ntchito malowo
3. Nthawi yeni yeni yogwiritsira ntchito malowo
4. Ndalama zingati zofunika kulipira ku malowo
5. Njira komanso nthawi yolipirira
6. Nthawi yeni yeni yomwe mungazapangire kumano kukozerera mtsokhano

7. Zina: kodi ntengowo ukuphakinziraposo magesi, gome, malo owonjedzera, zimbuzi komanso okonza pamalopo?

### **MATSIKU A MSONKHANO**

Matsiku a mtsonkhano atha kukhudziwa ndi malo omwe mwasankhawo. Antha kupezeka kuti ali opezeka matsiku ena kapena miyedzi ina. Zinthu zina zomwe zikuenera kuwunikiridwa posakha matsiku:

**-kusitha kwa Nyengo:** ngati mtsonkhano ungakachitikire panja, mukuyenera kuganirizira kuti kuli mphepo, mvula kapena kotetha ndipo mukuyenera kupewa izi. Mukuyenera kuwafunsa anthu okhala mu deralo ngati mtsokhano wakozedwa munyengo yoyenerera kuti ukachitike.

**-Matsiku Atchuthi:** Mukuenera kupewa nyengo ya ntchuthi chifukwa mabanja ambiri amakhala ali otangadidwa ndi kusangalala ndi achibale awo.

**-kuphatikiza mitsonkhano:** chepesani kuphatikitsa mitsonkhano yanu ndi yamu derayo monga zikondwerero, zaku sukulu komanso mitsokhano ya ndale.

### **NTHAWI YA MTONKHANO**

Kuti mukafikire anthu ambiri, mukapange mtsonkhano nthawi yonena kuti antha kubwera. Lingalirani mmene amagwirira ntchito anthu am'deramo.

### **KUFALITSA UTHENGA WA MSONKHANO**

Ngati mungalephere kudziwitsa anthu za mtsonkhano, musemphana ndi kuthekera kumwe nkumano wa anthu ambiri umakwaniritsa. Ngakhale ndi ndalama zochepa, mutha kufikira dera lalikulu ndi nkhani yankumanowu. Choyamba mukaziwe zinthu ziwiri izi:

1. Zoyenera kuyika polengezetsa.
2. Komwe mungagwiritsire ndalama zomwe ziripozo.

Tiyeni tilingalire zinthu izi:

### **ZOMWE MUNGAYIKE:**

Matsiku, nthawi komanso malo eni eni amene mukapangire mtsonkhano ayikidwe mukulengedza kwanu. Awuzeni anthu kuti Yesu akadachitabe zozizwa za chipulumutso, machiritso komanso kumasula matsiku ano. Ichi chimapereka chilakolako kwa amene akufuna machiritso kapena kumasulidwa kapenaso ali ndi abale awo amene akufunikira zinthu izi. Zimabweretsanso anthu ku mtsonkhano ndi mzimu wachiyembekedzo, pofunafuna kuwonekera kwa mphamvu ya Mulungu.

### **KUMENE MUNGAGWIRITSIRE NTCHITO NDALAMA**

Izi ndi njira zina zolengedzetsera zomwe mukuenera kuunikira pomwe mukugwiritsa ntchito bajeti yanu yakufalitsa uthenga:

**Timapepala toitanira:** Timapepala toitanira nditofunikira kwambiri polengedzetsa mtsonkhano omwe mungakonze. Kulengedza mtsonkhano munjira iyi muntha kugwiritsa ntchito ndalama zochepa chifukwa pepala imakhala yaying'ono yokwana mainchesi



pafupifupi  $5\frac{1}{2}$  ndi  $8\frac{1}{2}$ . Zinthu izi zitha kuperekedwa pamanja m'misewu, malo azamalonda, ndi malo ochedzerapo. Zintha kuperekedwa kwa okhulupira amu deralo komanso mipingo kuti igawe kwa anthu. Muthanso kugawa poyenda khomo ndi khomo. Timapepalati katipangeni topereka chikoka, koma tosalowa nthumba kuti tikakhale tambiri. Kawonetsetsemi kuti mwapasa nthawi yayitali anthu opanga timapepalato kuti akapange tochuluka panthawi yomwe mudzatifune.

Kagaweni timapepalati kumadera onse amene mukufuna kufikira sabata imodzi msonkhano usanayambe. (Madera amene kungakhale zotsutsa zambiri, ndichithu chamzeru kuti mukagawe mapepalawa kutasala matsiku atatu kuti mupange mtsonkhano.) Pangani magulu a anthu kuti apite m'madera onse akagawe timapepalato. Njira yoyenera kuchita ndikuwapasa anthu mapu a deralo powatumiza mitsika yosiyana siyana.

**Lembani pachinsalu chachikulu:** Ichi ndichinsalu chomwe chingayikidwe pakati pa mzinda. Muonetsetse kuti msewu waukulu wolowere mu mzinda mwayika chinsaluchi. Ndkoyenera kwambiri kukapepha chiroledzo kuchokera kwa akuluakulu a mzindawo. Muthanso kuyika chinsaluchi mu malo azamalonda ndi malo komwe anthu amakachedzera—malo amene anthu ochuluka makumanapo. Muonetsetse kuti uthenga onse (matsiku, nthawi, malo) zalembedwa pa chinsalupo.

**Maposita:** Maposita amakhala akulu kuposa timapepela toitanira, amapangidwa mofanana ndi uthenga ofananaso. Kusiyana kwake ndikoti maposita amakhala aakulu komanso amalembedwa pa mapepala olemera kuti ikayikidwe malo onse opezeka anthu madera onse. Ndishoyeneraso kupanga gulu la anthu ndikuwauza malo oyenera kukayika kaposita amenewa. Cholinga ndichofuna kuyika maposita pomwe anthu angathe kuona, pamene pamayenda anthu ambiri. Musayike posita imodzi pa malo. Anthu ambiri amakopeka ndi malo omwe maposita ayikidwa ambiri.

**Chinkuza mau:** Pali anthu ena omwe sangathe kuwerenga, mapepala, maposita kapena pachinsalu koma angathe kuvetsetsa pemene mukulengedzetsa pachinkuza mau. Mosamalitsa lembani uthenga wanu kuti mudziwerenga pamene mukulengedzetsa. Pewaninso kubwereza bwereza dera limodzi pamene madera ena musanafikire.

**Nyuzipepala:** Uthenga wamu nyuzipepala ukakhale ndi uthenga omwe mwayika pa timapepela komanso maposita aja. Musachite mantha kunenerera, chifukwa mukugwira ntchito yothandidza mzinda. Anthu akapulumsidwa ku mankhwala ozundudza ubongo, mowa, kuchiritsidwa misala komanso matenda ena akuthupi kudzera ku mtsonkhanowu. Madera akakhala abwino chifukwa cha ntchito ya Mulungu yomwe ikuchitika mmaderawa. Nyuzipepala zina zitha kulengeza nkhani imodzi ya msonkhanowo mwaulere. Nkhaniyi mukayikemo matsiku, nthawi komanso malo eni eni ankumanowo, koma uthengawu ukakhala ndi mfundo zambiri kuposa mauthenga onse.

**Makina a intaneti:** Ngati muli ndi mwayi okwiritsa ntchito intaneti, gwiritsani mwayiwu polengedzetsa uthengawu.

**Nyumba za kanema komanso zowulutsa mawu:** Ngati nyumba zowulusira mawu komanso za kanema ziripo zambiri muderali, linganirani kugwiritsa njira iyi. Osayiwalala kuti mukugwira ntchito ya chifundo, ndiye osaopa kunenerera. Mukaonetsetse kuti

mwalemberana gwirizano wanu umene ukukamba za tsiku komanso kuti dzitenga matsiku angati kuti mtsonkhano uthe.

Izi ndi njira zina zomwe mungagwiritsire nyumba zowulutsira mawu otsalipira ndalama:

-Lumikidzani ndi munthu komanso bungwe limene limawulutsa zinthu za chikristu pa Radio kapena pakanema, ndikuwauza kuti akulengedzetsereni za chitsitsimutso chanu.

-Afunseni kuti azabwere ku msonkhano woyamba ndikuuwulutsa mtsonkhanowo.

-Afunseni kuti ngati inu m'busa yemwe mwayenedera deralo, azakufunseni mafunso pa pologalamu imodzi mwa ma pologalamu omwe amaulusa.

**Mauthenga apadera dera:** mauthenga apadera dera atha kupita ku boma komanso ku akulu akulu azamalonda ndi akuluakulu ena aderali.

**Kulengedza kwapa kamwa:** kulengedza kwapa kamwa kutha kuchitikira: komwera mowa, m'masukulu, ku zochitika za m'mudzi ndi m'makachisi.

### **CHUMA CHAPA MTSONKHANO**

Ndidzoleredwa kutorera chopereka pa mtsonkhano, ngati ziri chochi, chopereka chitoleredwa kumapeto kwa mtsonkhano; osati tsiku loyamba. Choyamba, mphamvu ya Mulungu ikuyenera kutenga dera lonse kuti mukagwire mitima yambiri ya anthu. Anthu akazizwa zeni zeni za Yesu Khristu, mphamvu za adani kuzera kumabodza, kugona kapena ma umboni abodza ukhuzana ndi zachuma sizingasokonedze ntchitoyo.

Zachuma zonse zikachitike aliyense akuwona. Kutu zikhale choncho, ndikoyenera kuti mukasakhe akulu akulu okhulupirika kuti akayendese za chuma. Kuwerengera, kulembera komanso kusunga ndalama kusakasiyidwe m'manja mwa munthu modzi. Anthu osachepera atatu akakhalepo pamene chopereka chiziwerengedwa ndikusungidwa. Ngati pali palo otsungira ndalama pafupi, ndikoyenera kutsegulako buku ya mtsonkhanowo.

Ndandana onse wa zachuma momwe wayendera ulembedwe ndi kusungidwa, zomwe mwalandira komanso zomwe mwagwiritsa ntchito. Chiri chonse chikakhale ndi chiphaso, ndipo m'mene zinthu zonse zayendera zikaperekedwe kwa azibusa ndi ku mipingo yonse imene inatenga nawo gawo. Chopereka chikagwiritsidwe ntchito pochitira izi; kulipira pamalopo, kulengedzetsa mtsonkhanowo, kubwerekera zida za nyimbo, kulipirira mayendedwe, malo ogona komanso zina zokugwa mwadzidzidzi.

### **KUKONZA PAMALO OCHITIRAPO MTSONKHANO TSIKU LISANAFIKE**

Pali zinthu zambiri zoyenera kukonza pamalo a mtsonkhano tsiku loyamba litsanakwane. zinthuzo ngati izi:

#### **MBALI YA MALOWO:**

Mbali zonse zapamalo ochitikira mtsonkhano mukuyenera kuyika maposita, zinsalu zija komanso zizindikiro pa bwalopo ndimalo ena odzungulira.

#### **MALO A NSANJA:**

Ngati pamalopo palibe nsanja, mukuenera kumanga nsanja imodzi. Choyamba kuchita ndikuona kale malowo. Mukuyenera kuyang'ana zinthu izi:

1. Kodi anthu azatsendera ku nsanja kusatengera kuchuluka kwa anthu? Ngati mulibe zotchinga mbali komanso kumbuyo kwa nsanja, ndiye kuti anthu azakhala mozungulira bwalo ndipo kuzakhala kovuta kuti anthu muwakodze ndikusungaso chidwi chawo.
2. Ngati mtsonkhano ukuchitikira mkati mwampanda kapena pali chotchinga chirichose, ndikofunikira kuti nsanja yanu muyimange kutali ndi khomo lolowera kuti anthu asalalowera ku nsanjako kupewa kusokoneza mtsonkhanowo.
3. Ngati bwalolo siili pamalo abwino mukuyenera kumanga nsanja yanu pamalo pomwe anthu angaone bwinobwino. Ngati pamalopo palibe malo oti anthu angakhale, anthu akuyenera kuyima pamene mtsonkhano ukuchitika koma ndizovuta kuti anthu akayime malo otserereka.
4. Ngati mukupangira pa malo ochitira malonda kapena malo ochedzera, mukuyenera kumanga nsanja yanu kumalo kumene kulibe phokoso lambiri lama galimoto. Munthawi ngati iyi, kampani yopanga matabwa imatha kupereka matabwa kuti mumangire nsanja yanu ya mtsonkhano. Nthawi zina, atha kukubwerekani kapena kukukongozani. Ichi ndichabwino kuposera kugula chifukwa mukabwedza mukamaliza. Muthanso kuyika nsanja yanu pamwamba pama pipe akulu akulu amafuta kapena mapipe amadzi ngati alipo. Kukula kwa nsanja kumatengera ndi anthu amene mukufuna kuti abwere. Muwonetsetse kuti mwayika linga kulunjika ku nsanja mbali zonse. Izi zikagwira ntchito pa nthawi ya: umboni wachipulumutso, machiritso komanso kumatsulidwa amene mudzawatenge mu khamu la anthu. Kansewu kolimba koyenda mbali mbali mwa linga ndikothandiza kwambiri koti kamathandizira kuyenda bwino bwino. Kansewu kakang'ono kamatabwa kokhomedwaso bwino kulunjika ku linga kamathandiziranso mayendedwe abwino.

#### **MALO A GUWA:**

Mumange chingwe kutsogolo kwa nsanja. Izi zimachepetsa anthu kudzada kutsogolo ndiposo zimapereka malo oti anthu ayimepo amene akufuna kulandira Yesu. Kodzani chingwechi kuti chitha kugwesedwa pamene mukufuna anthu onse abwere kutsogolo omwe akufuna kulandira Yesu.

#### **MAGETSI:**

Kawonetsetseni kuti mwalekanitsa komwe mukutenga magetsi ndi thambo dzina. Mthambo zonse zisachokera gawo limodzi. Nthawi zonse ndikochokera magetsi ndi malo oyatsira ndikudzimitsira magetsi akhale pambali pomwe anthu sangasokonedzepo.

#### **ZIMKUDZA MAWU:**

Kayetseni zimkudza mawu moyenera nthawi ya mtsokhano isanakwane. Ndizothandiza kukhala ndizina pambali zodikirira kuti zina zikawonongeka mutha kugwiritsa zina.

#### **SUNGANI MALO:**

Yikani zizindikiro zowoneka pa malo omwe mwasunga. Chitsanzo, mwina mwasunga malo a omwe azatanthaunzire kwa amene samamva chiyankhula china. Mukuyeneraso kukhala ndi malo ena okhalako oyimba pa patsonkhanopo. Mukuyenera kusunganso malo a anthu ogwira ntchito.

## **KUPHUNZITSA ANTHU OGWIRA NTCHITO PA MTSONKHANO**

Kuphunzitsa okhulupirira amu derali kuti azathandize pa mtsonkhano, zimathandidza kuti asazakhale anthu ongowonerera. Amakhali mbali imodzi yokafikira miyoyo ndi kupemphera anthu.

### **KULEMBA OGWIRA NTCHITO:**

Ogwira ntchito pamtsonkhano akuyenera kukhala okhulupira okhwima ochokera mipindo yozungulira komwe kudzachitikire mtsonkhanowo. Azibusa atha kugwiritsidwa ntchito kuti asankhe anthu ogwira nthito. Ngati komwe mukupangitsa mtsonkhanoko kulibeko mipingo, lembani ntchito okhulupirira ochokera m'madera ozungulira kuti abwere kuzathandidzira mtsonkhano ngati ogwira ntchito.

### **MATSIKU AKUPHUNZITSA NTCHITO**

Ndichabwino kuti ogwira ntchito akaphunzitsidwe kutasala matsiku awiri oti mtsonkhano uchitike pakuchita izi zikathandidzire kuti anthu aja zikakhalebe ziri m'mutu mwawo. Phunziro loyamba lintha kuchitika ku mpingo kapena ku holo, koma phunziro lomalandiza likuyenera kukachitikira pa bwalo pomwe mutachitire mtsonkhano kuti anthu akayikidwe malo awo oyenera.

Chifukwa chakuti munthu wakhala khristu nthawi yayitali sizikutethauza kuti sakaphudzitiswayi. Musalole munthu kukanena kuti, “ndikuziwa chimene mukufuna kuti chichitike, ndiye sindikuenera kupanga nawo ma phunziro”. Onse ofuna kutenga nawo gawo kaya azibusa kaya okhulupira ena onse akuyenera kuphunzitsidwa.

### **KUKODZEKERETSA ANTHU OGWIRA NTCHITO:**

Ndichotheidza kuti anthu ogwira ntchito pa mtsonkhano adzavale zinthu zoti anthu azawazindikira mwachangu monga, ma baji kapena ma riboni amitundu mitundu. Awuzeni kuti azavale mowoneka bwino, ndi kumagwira ntchito ndi munthu wantundu wawo (mwamuna kuthandidza mwamuna dzake ndi nkadzi kuthandidza nkadzi nzake). Azafike mwachangu ola limodzi mtsonkhano usanayambe.

Ogwira ntchito akuyenera kupasidwa ma Baibulo, zolemba ndi ma khadi, ngati mukuwagwiritsa ntchito yolembe mayina komanso komwe amakhala anthu omwe alandira Yesu kumene. Ngati ndalama ziripo, ndizofunika kuti mupangitse zinthu zomwe azikawerenga anthu akapita kwawo monga Uthenga Wabwino wa Yohane kapena mathalakiti omwe angapezemo malangizo a moyo wachi Khristu.

### **KUPHUNZITSA ALANGIDZI:**

Ogwira ntchito akuyenera kpatsidwa malandizo a uphungu. Akuyenera kudziwa mmene angamulandiritsire munthu Yesu Khristu komanso mmene angapempherera omwe akufunikira kumasulidwa ndi machiritso. Gwiritsani ntchito magawo osakhidwawo mu phunziro ili kuti muwaphunzitse madera amenewo. Mulinsu ndondomeko yina yowonjedzera yomwe ingakuthandidzeni mu phunziro iri.

Ogwira ntchito akatumikira kwa osapululumuka pamene akufuna kulandira Yesu Khristu. Athaso kuyitanidwa kuti akatumikire anthu omwe ali ndi ziwanda (onani mmene

mungakhazikitsire bata). Amathandiziranso kutumikira machiritso ndi kumasula anthu pamene akugwira ntchito malo omwe ayikidwa pamene inu mukupepherera anthu ena.

### **KUNKHAZIKITSA BATA:**

Kumbukirani kuti muli mu nkondo ya Uzimu ndi miyoyo ya abambo ndi azimayi, kuwapulumutsa kutsogolo lawo lopita ku Gehena. Pamene mukuchita izi pa nkhamu la anthu, mphamvu zakumidima sizikhala chete kumangoonera.

Choyamba, mukuenera kukhala ndi mphamvu komatso ulamuliro wa Mzimu Woyera kuti mukamange mizimu yaziwanda zofuna kusokonedza. Chachiwiri, perekani ntchitoyi kwa ogwira ntchito anu. Akuyenera kukhala atcheru ku chisokonedzo ndi zinthu zosokonedza ndiposo akadziwe chochita zinthu izi zikachitika.

Aphunzitseni kuyenda mwachangu komanso asamanyodzere vuto likagwa. Musadikire kuti dzithu zichitike mwa idzo zokha, chifukwa sizichitika. Musadikire kuti munthu wina achite. Zindikirani mwasanga kuti ndintchito ya m'derekedzi ndikuthana nayo mwachangu.

Chofunikira apa ndikuthana ndivuto munjira yoti simubweretsa vuto lalikulu kupotsa lomwe lachitika kale. Musapange chinthu chomwe chingakulitse vuto. Chitani munjira yomwe mungabwezere anthu malingaliro awo ku nsanja mwasanga sanga.

Nthawi zambiri, Satana akagwiritsa ntchito munthu woti ali ndi ziwanda kuti abweretse chitsokonedzo. Njira ina, ogwira ntchito sakuyenera kuthana nacho chiwandachi pakati pa guru, koma amutenge munthuyu mwachangu kupita naye kunjira kwa bwalo ndikukatulutsa chiwandachi. Chofunika ndichoti, chirichose chochitika, chikachitike mwachangu komanso modekha. Kadzindikireni zitsokonedzo kuti ziri motani: Satana kuntchinga chimene Mulungu akuchita.

Ngati mbali imodzi yokhazikitsa bata, mukuyenera kuphunzitsa anthu apadera dera ogwira ntchito ku nsanja komanso ndi linga dzake. Anthu ogwira linga asalole kuti anthu osavomeredzedwa kuti abwere ku nsanja, komanso athandize anthu ovomeredzedwa kupita komanso kubwera ku nsanja. Komanso akalandira anthu amene abwera ndi maumboni kuchokera ku khwimbi la anthu omwe abwera ndi ogwira ntchito, akasimikidzadi zozizwa ndikuwaperekedza ku nsanja.

Anthu ogwira ntchito ku nsanja akuyenera kukhalaso ma asha omwe akuyenera kuyikidwa mbali zonse za nsanja, amene aphunzitsidwa kuti asalole wina aliyense kubwera ku nsanja ngati sanatumidwe ndi osunga linga. Komanso anthu awiri ogwira ntchito ku nsanja akuyenera kupedzeka pothandizira kuti mzere wa umboni udziyenda mwadongosolo.

Ngati gawo limodzi lusungitsira bata, mukuenera kuwaphunzitsa ma asha kuti azithandiza anthu, kuwapasa malo kapena kuti mwina akuchoka papando (ngati malo aperekedwa) ndipo chokera kopereka chopereka. Mukueneratso kuwaphunzitsa ogwira ntchito kuti akathandize anthu amene abwere ndimagalimoto kuwaunikira mmene akasungire magalimoto awo. Mukuenera kuyendera malo osungira galimoto ndi kuonaso mmene magalimoto azayimire. Mukueneratso kusunga malo osungire magalimoto a anthu ogwira ntchito komanso aliyese akutenga gawo pa msonkhano. Ikani zizindikiro zoyenera kumalo osungira magalimoto, magesi oyenera ngati kuli kotheka komanso yikani alonda kuchitira anthu owononga (kumbukirani kuti muli mu nkondo ya Uzimu).

## CHIPULUMUTSO:

Pamene mukuyitana anthu kuti alandire Yesu kristu, ogwira ntchito akuyenera kuphunzira kuyima mwachangu ndikunyamuka kupita ku gowe malingana ndi mmene munawagawira. Kulandiritsa anthu Yesu Kristu zimaonetsa kuti ndimbali imodzi ya kulalikira pa mtsonkhano. Aphunzitseni kuti malingaliro awo akayike kudzimene mukuyankhula pa nthawi imeneyi. Mulungu atha kukutsogolerani kuti mukatumikire mosiyanasiyana malingana ndizomwe zikuchitika, akuyenera kukhala okodzeka kukayenda nanu pamene Mzimu Woyera amakhala akuyenda pa nthawiyi.

Nthawi zina, chifukwa kwakuchuluka kwa anthu, ndikoyenera kuti mukapemphere pemphero la gulu ndipo mukaonetsetse kuti anthu akubwereza pambuyo panu pephero la anthu ochimwa kuti akakhulukidwe machimo awo. Ndikoyenera kuti onse amalakhula pephero la chipulumutso akalondoledzedwe mosamalitsa, onetsetsani kuti zinthu zitatu izi mwa chimodzi chikachitike:

-Alangidzi akuyenera kulemba pa khadi yachitsankho, dzina la munthu ndikomwe amakhala za amene walandira Yesu kumene kuti Abusa amu derali azimuyendera.

kapena

-Mukuenera kuwauza kuti mamawa otsatira kuzakhala kukumana ndi anthu omwe amulandira Yesu Kristu.

kapena

-amene anabwera kumtsonkhano amatumizidwa kwa alangidzi apadera dera kapena malo ena pa bwalopo. Ogwira ntchito akuyenera kuwalondolela anthuwu, kuwapatsa malangidzo ena apadera komanso kutenga komwe amakhala polemba pa khadi ya chitsankho.

Ngati mwagwiritsa khadi ya chitsankho, lembani zinthu izi:

-Dzina

-Komwe amakhala

-Nambala ya phone

-Mene amvera: Malo owonesa kuti anabwera kudzalandira chipulumutso, kuzalimbikitsa ubale wawo ndi Yesu Kristu, anabwerera kumasulidwa kapena machiritso.

-Ndemanga: Malo omwe mungalembepe ndemanga ngati inuyo alangidzi, mulembe zomwe ziri zofunikira makafuna kuwasatira

-Kusayina: malo oti mulangizi alembepe sayini yake.

Ngati mwagwiritsa ntchito makhadi ya chinsakho, muwagawe magawo awiri, ngati ziri zotheke, kaboni amapangidwa pamene pepala likulembedwa. Pepala leni leni ndilomwe abusa azasatire poyendera anthu. Pepala lina lithanso kutengedwa ndi ogwira ntchito kuti akayendere anthu amene alandira Kristu kumene. Aphunzitseni ogwira ntchito kuti azilemba zowoneka pamakhadi. Lembani munthu yembe akhale ndi udindo otolela makhadi komanso kunsunga makhadi.

## **MACHIRITSO NDI KUMASULIDWA:**

Kuwonetsera kwa Mphamvu ya Mulungu kumatsimikiza kulalikira Uthenga Wabwino. Mmene muzikaphunzira pa mutu 2 waphunziro ili, mukaziwa kuti machiritso komanso mamasulidwe ndi ofunika kwambiri mu kulalikira. Kuti mukakweze chikhulupiriro cha ophunzira, werengani mawu a Mulungu, kuti mukakope osakhulupirira, ndichothandidza kuti mukapereke maumboni azimene Mulungu akuchita pa msonkanopo. Ziwani kuti anthu osapulumsidwa amabwera asakuhulupirira. Ndi ovuta zedi. Kufikira ataona Mphamvu ya Mulungu, ndipamene amakhulupirira.

Pamene mukupepherera machiritso komanso mamasulidwe, muwauze ogwira ntchito kuti azipephera akuyang'ana. Pamene mukupemphera awuzeni anthu onse kuti ayike dzanja lawo pamene akumva kuwawa. Mukamalidza kupephera awuzeni anthu kuti achite zimene samatha kuchita. Awuzeni ogwira ntchito kuti akaone anthu pamene akuyika manja awo pozowawa zawo ndipo pemphero likatha akachite chite ndichikhulupiriro. Ogwira ntchito ayendere anthu aja ndikutenga maumboni awo.

(Pamene mukuphunzitsa ogwira ntchitowa, pempherani pemphero lamachiritso komanso lamamasulidwe. Nthawi zambiri machiritso amatha kumachitika pamene mukuwaphunzitsa.) Pamene mukawaphunzitsa anthu awuzeni mmene angamuwonere munthu osawona pogwira dzala ndikuwauza kuti awerenge. Kwa osamva, phokoso litha kupangidwa kuchokera kumbuyo kwake, ngati kuomba manja kangapo. Machiritso owoneka ngati, osamva, osaona, osakula, opuwala ziwalo, alimbikitsa chikhulupirira kuposera machiritso amkati omwe simungawadziwe nthawi yomweyo.

Pamene ogwira ntchito apeza munthu yemwe wamasulidwa kapena kuchiritsidwa, awuzeni kuti amubwerese munthu (osati kumutumidza) kwa anyamata omwe apanga linga kutsogolo. Kenako anyamata apanga linga lija amuperekedze munthu uja ku nsanja kumeneko mutha kuwafunsa mafunso komanso kugawana umboni wawo wa zomwe Mulungu wachita. Kenako ogwira ntchito abwerere kumalo kwawo ndikukapitiridza kulandira anthu ndikumva ma umboni awo.

## **KUGAWA MALO PA BWALO:**

Mukuyenera kujambula malowo tsiku loyamba la maphunziro anu ndikuwawonetsa ogwira ntchito malo omwe azayime pogwira ntchito tsiku la mtsonkhano. Tsiku lachiwiri la maphunziro amane atakachitikire pa malo omwe mukachitire mtsonkhano, mukuenera kuwayika malo awo amene azikagwirira ntchito tsiku mtsonkhano.

Mukakhale ndi anthu ambiri ku guwa omwe angathe kugwirana manja ndikupanga mzere wa manja. Izi zimathandidza kukhazikitsa bata komanso potumikira anthu amene abwera kutsogola.

Ikana anthu amene mwawaphunzitsa kupanga linga komanso anthu ogwira ku nsanja mmalo awo oyenerera kenako agaweni anthu ena osalawo mmalo onse odzungulira pamalopo. Onetsetsani kuti mwayika anthu ogwira ntchito pakhomo polowera komatso potulukira kuti mukatetedze magetsi.

## **KUCHITITSA MTSONKHANO**

Awa ndimagandidzo omwe mungapangire mtsonkhano:

### **KUYAMBA MTSONKHANO:**

Ikani nyimbo zapamwamba zomwe zikalire kwakathawi monga phindi 30 mtsonkhano usanayambe. Nyimbo zikakopa anthu kobwera kumaloko komanso zikakozekeeretsa mitima ya anthu omwe abwera kale kuzalandira Mawu a Mulungu. Awuzeni oyimba nyimbo komanso otsogoleri nyimbo za nyimbo zomwe angayike. Sankhani nyimbo zomwe ziri zachikoka, zotsitsimutsa komanso zotumikira. Musasankhe nyimbo zovuta kuvetsetsa. Nsankhani nyimbo zomwe zikupereka moyo komanso chirimbikitso zomwe zingawapase chikoka anthu osapuluma.

Ukatha utsiku oyamba, mudzakhala ndi anthu omwe apulumutsidwa, kuchiritsidwa komanso kumatsulidwa. Awuzeni ena mwaiwo kuti azayikire umboni kwa phindu 30 musanayambe mtsokhano. Chezani nawoni komanso afunsi mafunso kupewa kuti wina angalowero (njira zina za satana zofuna kusokonedza).

### **KULALIKIRA MAWU:**

Panthawi yoyikika, yambani msonkhano. Ikani nthawi yochepe yazochitika zina. Cholinga cha msonkhano ndikufikira miyoyo yambiri kwa Ambuye. Kuchita izi, Mawu a Mulungu akuyenera kulalikiridwa komanso Mphamvu ya Mulungu iwonekere. Anthu abwera ndi mizimu yambiri, matenda komanso zovuta zina. Sanabwere kuti azave zolengedza zazitali, nthabwala, kufotokoza komanso kucheza kopanda phindu.

Musanayambe kulalikira, awuzeni anthu kuti mupempherera machiritso, kumasulidwa pakutha kwa mtsonkhano. Anthu ambiri amabwera kudzachiritsidwa, mukayamba kulalikira popanda kunena izi amawonga ngati sananve cholinga cha mtsokhanowo. Mukawauza mosindika kuti mupempherera odwala kumapeto, adzalandira uthenga wanu mwantcheru.

### **PEPHERO LACHIPULUMUTSO:**

Pomaliza kulalikira, choyamba kuchita chikakhale chipulumutso. Ziwani kuti machiritso a mizimu ndiwofunikira kwambiri kuposa machiritso a thupi. Mupempherera matupi awo, koma choyambirira ndikupempherera mizimu yawo kuti Mulungu awachiritse muzimu ndikuwakhulukira machimo awo kudzera mwa mwadzi wa Yesu Kristu.

Nthawi zina, chifukwa kwakuchuluka kwa anthu, ndikoyenera kuti mukapemphere pephero la gulu ndipo mukaonetsetse kuti anthu akubwereza pambuyo panu pemphero la anthu ochimwa kuti akakhulukidwe machimo awo. Ndikoyenera kuti onse amalakhula pemphero la chipulumutso akalondoledzedwe mosamalitsa, onetsetsani kuti zinthu zitatu izi mwa chimodzi chikachitike:

-Alangidzi akuyenera kulemba pa khadi yachitsankho, dzina la munthu ndikomwe amakhala za amene alandira Yesu kumene kuti Abusa amu derali azimuyendera.

kapena

-Mukuenera kuwauza kuti mamawa otsatira kuzakhala kukumana ndi anthu omwe amulandira Yesu Kristu.

kapena



-amene anabwera kuchipulumutso amatumizidwa kwa alangidzi apadera dera kapena malo ena pa bwalopo. Ogwira ntchito akuyenera kuwalondolela anthuwu, kuwapatsa malangidzo ena apadera komanso kutenga komwe amakhala polemba pa khadi ya chitsankho.

### **MAPEMPHERO AMACHIRITSO KOMANSO AKUMASULA:**

Kusatira pemphero lachipulumutso, ndinthawi yoti muyambe kupempherera machiritso komanso mamasulidwe. Nyengo za kulalikira ndizosiyana, nthawi zina Mulungu atha kukutsogolerani mwanjira yina mmene mungatumikirire. Awa ndimaganiidzo ena amomwe mungatumikirire machiritso pamalo a mtsonkhano.

Pakati pa nkhamu la anthu, tsizotheka kuti mukapempherere modzi modzi. Choyamba, pempherani mapemphero otsiyana tsiyana molingana ndi matenda a anthu. Awuzeni ogwira ntchito kuti abwerese ma umboni ku nsanja kuchokera kwa omwe alandira machiritso. Chikhulupirira cha anthu chikakwezedwa ndima umboni amenewa, kenako mukapemphere pemphero lomalizidza lomatsula mitundu yonse yazowawa. Kumbukirani kuti, zofunikira kuti mukalore kuti Mulungu atsogoleri pamalopa. Palibe dongosolo liri lonse lingatsatidwe.

### **KUTSEKA MTSONKHANO:**

Pakutseka mtsonkhano, onetsetsani kuti mwalengedza za mtsonkhano wpsatira ndi nkumano wa mmawa omwe utachitike ndi amene alandira Khristu kumene. Perekani dongosolo omveka bwino ngati nthawi komanso malo okumana.

### **KUTSATIRA OTEMBENUKA MTIMA**

Aliyense amene walandira Yesu akuyenera kuyenderedwa mwapadera dera. Izi zimakwaniritsa “kuphuzitsa zinthu zonse.”

Pamene anthu abwera pa gome kuzalandira Yesu Kristu, chinthu chimodzi mwa ziwiri izi chimachitika:

1. Olandira Yesu kumene alembe pa khadi ya chitsankho: Izi zimachitikira pa gome kapena muchipinda cholangidzira. Ma khadi awa aperekedwe kwa azibusa amadera kuti mwina awayendere anthuwo.
2. Tsiku lamaphunziro kwa anthu omwe alandira Yesu linedwe: panthawi yama phunziro a m'mawa anthu omwe alandira Yesu akuyenera kuyenderedwa mwapadera dera komanso mayina awo ndikomwe amakhala kutengedwe kuti mukapitiridze kuwayendera.

Cholinga chowayendera chikhale pamutu woti “Musayataye.” Musawataye anthu amene alandira Yesu kumene kufikira atakhazikika mu mipingo yamudera lawo.

Mutu 13 waphunziro iri ukunena momwe mungawayendere ndikuwaphunzitsa okhulupirira atsopano.

## MAFUNSO OZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera

---

---

---

2. Fotokozani phindu la mtsonkhano wa uvangeli.

---

---

---

---

3. Yakhani padera, lembani mwachidule mfundo zomwe zakambidwa muphunzirori zokhuzana ndi:

- Kukonzekera mu Umzimu
- Dera lopangira Chitsitsimutso
- Mgwirizano wa malo
- Tsiku ndi nthawi
- Kulengedzetsa
- Zachuma
- Kukonzekera kwa zogwirira ntchito
- Kuphunzitsa ogwira ntchito
- Kuchititsa mtsonkhano
- Kulondoloza

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

## ZOONJERA POPHUNZIRA

1. Izi ndizoyenera kutsatira pamene mukuphunzitsa anthu anu mmene angalangidzire anthu amene akufuna kulandira Yesu Kristu:
  - (1) Zifotokozeni nokha (ngati mlangidzi) kwa munthu amene wavomeredza kulandira Kristu
  - (2) Afunseni dzina lawo ndipo mukalemba kuti musayiwale zomwe mwakambirana. (ngati agwiritsa khadi ya chitsankho, lembani zonse pa khadipo. Ngati simunagwiritse lembani papepala basi.)
  - (3) Afutseni kuti, “chifukwa chimene anakwedzera dzanja (kubwera kutsogolo) utsikuwu?” Izi zikapereka mwayi kuti munthuyo akuwudzeni zosowa zake kwa inu.
  - (4) Sizingatheke kuti mukamuyankhe munthu funso liri lonse lomwe wafunsa, koma mawu a Mulungu amakhala ndi yankho kufunso liri lonse. Ngati mwakumana ndi funso kapena zovuta ziri zonse zomwe simundakwanitse kuyankha, itanani abusa kapena munthu wina akuthandidzeni.
  - (5) Musamukakamidze munthu kuti apange chitsankho. Lolani Mzimu wa Mulungu ugwire ntchito yake.
  - (6) Mukapedza chosawa cha munthu mukumulangidza uja kudzera mukukambirana kwanu paseni langidzo kuchokera mu Mawu a Mulungu ndikupemphera naye. Ngati wavomeredza kulapa, musogolereni ku pephero la anthu ochimwa ndikupempha chikhululuko chamachimo ake ndikuvomeredza Yesu Khristu kuti ndimpulumutsi. Langidzo lanu likakhale losavuta. (Musakayesere kumuphunzitsa ziphunzitso za chikhulupiriro cha a Krhistu mukathawi kochepe!) Ngati akufuna machiritso kapena kumasulidwa, tumikirani madera amenewo.
  - (7) Apatseni olangizidwawo zinthu zomwe mwapatsidwa kuti akagwiritsire ntchito imeneyi, monga za Uthenga Wabwino wa Yohane kapena mathalakiti amene akukamba za Umoyo wachi Khristu.
  - (8) Mukamaliza kulalikirara munthuyu, malizitsani khadi yachitsankho. Mulembe komwe amakhala ndi nambala ya telefoni. Lembani ndemanga iri yonse yomwe ingakhale yothandiza pamene muzamuyendere munthuyo.
  
- \*Dziwani: Pamene mukuphunzitsa ogwira ntchito, mutha kukambirana ndemanga zofanana zomwe anthu amakhala nazo ndi mene mungathanire nazo. Mwachitsanzo, amene abwera kutsogolo kufuna machiritso, kutsimikidzika kwa chipulumutso, kumasulidwa ku nsinga zosiyanasiyana.
  - (9) Kaperekeni khani ya chinsakho kwamunthu yemwe watumidwa kuti adzatolerere makhadiwo. Ngati ma khadiwo ali ma gawo awiri, perekani imodzi inayo sungati kuti nanunso mukathe kumufikira munthuyo.
  - (10) Muyendereni munthuyo mumawola 48 oyambirira. Kamuwoneni mmene akukhalira. “Osawasiya” kufikira atapedza mpingo ndikukhazika.
  
2. Mutu uwu wakhazika pa njira zopangira mtsonkhano womwe choringa chake ndikuwina miyoyo ya anthu. Sizingatheke kukambirana njira zonse zomwe mungapangire

mtsonkhano. Muntha kuganidza kuti mupange, mitsonkhano, maseminala, zitsitsimutso, zoyimbayimba ndizina zambiri. Umu ndi momwe mungapangire mitsonkhano ina ya kulalikira:

(1) Khadzikitsani cholinga cha mtsokhanowo: Cholinga cha mtsokhano, seminala, zitsitsimutso ndichani? Ichi chikakuthandizani kupanga dongosolo lanu.

(2) Khadzikitsani matsiku komanso nthawi yake

(3) Nsakhani Dera. Mukuyenera kuwunikira zinthu izi posakha malo:

-Kukula kwake: Likuyenera kukhala lokwanira anthu omwe mukufuna kuzabwera.

-Mawonekedwe: malowo akuyenera kukhala ndimaonekedwe mukufuna pa mtsonkhano. Machitsanzo, mukufuna kuti pazabwere anthu ambiri kenako muzawagawe magulu, mukufunikira malo akulu okhala ndi chipinda china chachikulu komanso china chaching'ono. Ngatiso mudzaphike ndikugawa zakudya, mudzafunira kuti malowo mudzakhale kophikira.

-Dera: Malowo akuyenera kukhala komwe aliyense antha kufikirako komanso kukhale koyandikira komwe anthu amakhala omwe mukufuna kuti abwerewo.

-Dzitenga ndalama zingati: mukuyenera kugwiritsa ndalama zomwe mungakwanitse.

(4) Nsakhani gulu loyendetsa ndikugawa ntchito motere:

-Oyendetsa Wankulu: Oyendetsawo akatsogolera anthu onse kuntchito zawo ndikuyendetsa mtsokhano onse.

-Mmene ziyendere: mene zikayendere muyikemo izi:

-Zonse zomwe zikachitike tsikulo lisanafike: Atachite ndani nanga amaliza liti?

-Zizayenda bwanji patsikulo: Chizachitike ndichani, panthawi yanji pa tsiku la mtsonkhano?

-Zinthu zomwe muzagwiritse ntchito powayendera.

-Ndalama zamtsokhano: kuti mupeze ndalama za mtsonkhano, sakana ndalama, lipirani ma bilu, tengani chopereka chapa mtsonkhano komanso yitanani alendo olemekedzeka kuti apereke ndalama.

-Mene mungakodzere malowo: Pali zinthu zina zomwe mungagwiritse pomanga malowo: Pipando, nsanja, matebulo, poyikira chopereka, zinkuza mawu, gome, zida zoyimbira, zinthu zomwe mungagwiritse ntchito polangizira komanso polembetsera.

-Kulembetsa: kodi anthu alembetsa? Ngati ziri chocho, ndikatundu wanji azaperekedwe panthawi yolembetsa? Mzere olembetsera uzayenda bwanji? Kodi pazakhala kulipira anthu akamadzalembetsa? Kodi muzafuna polembapo potani? Muzafuna anthu antundu wanji?

-Kulengedzetsa: mudzalengedzetsa bwanji? Sankhani munthu yemwe azalengedzetse monga, kulemba makalata, kuyimba ma lamya, nyumba zoulusira mawu, pakanema, nyuzipepala, maposita, kulengedza mipingo yamu dera ndizina zambiri.

-Kulangidza: sakhani munthu yemwe akaphunzitse alangidzi kuti akathandize anthu mudzosowa zawo za uzimu. Alangidzi akadziwe kumulandiritsa munthu Yesu Kristu, mene

angapepherere odwala komanso kulalikirara mamasulidwe. Akapasidwe ma Baibulo, ma thalakiti ndi pomwe atakalebepo dzina ndikomwe amakhala kwa amene akufuna kuthandizika muuzimu. Makhadiwa akuthandizirani kuti mukawayendere pakutha pa mtsokhano.

-Mulendo olemekedzeka: kodi mudzakhala ndi mlendo olemekedzeka? Ngati zili chocho, mukuenera kukhala ndi munthu yemwe akuyenera kuwayimbira komanso kuwayitana, katengeni zoyenereza zonse kwa iwo mene zochita zawo akodzera, perekani mayendedwe ndi malo opumapo ngati zikuenera kutero, kawafikireni ndizofuna zawo zakuthupi pa nthawi ya mtsonkhano.

-Nyimbo: Sankhani mkulu oyang'anira nyimbo kuti apeze zida komanso anthu oyimba, osogolere akwaya, apangeso dongosolo la nyimbo zapadera dera ndikutsogolera mpingo poyimba.

-Kosungira ana: kodi mudzapereka malo ochenzera ana? Ngati ndichocho, sankhani munthu yemwe azakodze malo ndikusakha anthu ozasewera ndi ana.

-Zogulitsa: Ngati mukufuna kuzagulitsa ma Baibulo, mabuku achi khristu, matepi komanso chakudya, mukuenera kusankha munthu yemwe azizayang'anira mbali imeneyi.

-Ma asha: Sankhani munthu yemwe azayang'anira ma asha omwe azakhazika anthu pansu, kulandira ndikutolera zinthu, kutolera chopereka, kuthana ndimavuto onse ngati zosokoneza zomwe zimachitika pamtsokhano.

-Zinkuza Mawu: Ngati mukupangitsa mtsonkhano wawukulu, mukuenera kukhala ndi zinkuza mawu zabwino. Pakhale munthu amene akuziwa bwino bwino komwe mungazipedze zithu zabwinozi.

-Kujambula Uthenga Overa kapena Owonera: Mukufuna kuti muzajambule mtsonkhanowu? Ngati chocho, mukuenera kupedza munthu yemwe azizajambula, kupanga ma tepi, akatenge zofunikira zonse.

-Otenga nawo gawo: mukufunikira munthu amene azawayang'anire anthu onse otenga nawo gawo. Chitsanzo, mayendedwe, chakudya kapena pogona ngati kuli koteru, othandiza anthu mavuto ena komanso ozayakha mafunso panthawi ya mtsonkhano.

-Kuyendera anthu: Nthawi zonse nsakhani munthu yemwe akuyenera kuyendera anthu, kutolera zinthu zanu, kukodza pamalopo, kunyamula zida zoyimbira, kuthokoza anthu onse anakuthandizani ndikunsakhatso anthu ena kuti akayendere anthu omwe alandira Yesu kristu.

## CHAPUTALA 13

### ZISAKHO KAPENA OPHUNZIRA

#### ZOLINGA:

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba vesi yapa mtima
- Kufotokoza “kutembenuka”
- Kufotokoza “ophunzira”
- Lembani madera 6 a dongolosolo lomwe mungagwiritse ntchito poyendera anthu omwe atembenuka mtima
- Nenani malamulo 9 omwe Yesu amagwiritsa ntchito kwa ophunzira
- Perekani mwachangu njira zoyendera anthu atsopano
- Perekani njira zowonjedzera momwe mungawayenderere anthu otsapanowa.

#### MAVESI OTSOGOLERA:

**Atakhala kumeneko nthawi, anacoka, napita pa dziko la Galatiya ndi Frugiya m'dziko, nakhazikitsa akuphunzira onse. (Machitidwe a Atumwi 18:23)**

**Nalimbikitsa mitima ya akuphunzira, nadandaulira iwo kuti akhalebe m'cikhulupiriro, ndi kuti tiyenera kulowa m'ufumu wa Mulungu ndi zitsautso zambiri. (Machitidwe 14:22)**

#### CHIYAMBI

Nthawi zambiri mumamva za utumiki waukulu, koma mumamvesesa utumiki umene Yesu anawapasa omusatira ake?

-Kodi lamulo linali longotembunudza anthu?

-Kodi inali yongopangitsa chitsitsimutso basi?

-Kodi inali yongowina anthu kwa Ambuye kenako kupita ku dera lina mwachangu.

Tiyeni tiwerenge malamulo ake kachikenanso;

**Cifukwa chake mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera:**

**Ndikuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya panso pano. (Mateyu 28:19-20)**

Cholinga chinali chopita ku mitundu onse, kuwaphunzitsa Uthenga Wabwino, kuwabatiza kenako kumawayendera ndikumawaphunzitsa zonse zomwe Yesu Khristu analamula. Ntchito yolalikira siyinamalizike popanda kuphunzitsa mwapadera dera.

#### ZISANKHO KAPENA OPHUNZIRA?

Mitundu iwiri yaziphunzitsa yomwe imachitika mu ntchitoyi:

**Yoyamba:** Kuphunzitsa Uthenga Wabwino opereka chipulumutso kwa anthu. Anthu akuyenera kumva Uthenga Wabwino kuti akavomeredze, kulapa machimo ndikubadwa mwatsopano:

**Cifukwa chake mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: (Machitidwe a Atumwi 28:19)**

Okhulupirira atsopano amatchedwa “otembenuka.” Otembenuka ndi okhulupirira Mwa Yesu amene wabadwa mwastsopano kudzera muchikhulupiriro ndikukhala nawo mbali ya Ufumu Wa Mulungu.

**Chachiwiri:** Kulalikirira pakutha zokambirana. Pamene munthu waphunzitsidwa ndipo wabwera kwa Yesu, akuyenera kuphunzira mmene angamusatirire Yesu Khristu.

**Ndikuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya panso pano. (Mateyu 28:20)**

Utumiki waukulu umawonetsa kuti otembenuka mtima akuyenera kuuzidwa zonse zomwe Yesu analamulira. Kuchita izi kumatchedwa “Kuyendera kapena kuphudzitsa.”

Paulo anali otsamalitsa mmene amayendera anthu omwe atembenuka mtima kumene ndi mipingo yatsopano. Malemba akuti ana...

**..... coka, napita pa dziko la Galatiya ndi Frugiya m'dziko, nakhazikitsa akuphunzira onse. (Machitidwe a Atumwi 18:23)**

**Nalimbikitsa mitima ya akuphunzira, nadandaulira iwo kuti akhalebe m'chikhulupiriro, ndi kuti tiyenera kulowa m'ufumu wa Mulungu ndi zitsautso zambiri. (Machitidwe 14:22)**


#### **TANTHAUZO LA KUPHUNZITSA OPHUNZIRA**

“Ophunzira” ndi otembenuka amene akhazikitsidwa molingana ndi Chikhulupiriro chachi Khristu ndipo ndiwoyenera kuka tembenudza ena ndikuwa phunzitsa. Mawu oti “ophunzira” amatathauza kuti mwana wa sukulu, munthu amene akuphunzira posatira aphunzitsi. Ndizopotsa chiziwitso chabe. Ndikuphunzira kumene kumasitha moyo wa munthu. Kudekhesa sikungopereka fundo, koma ndikumuwumba munthu.

#### **MKOMBERO WA CHISANKHO/OPHUNZIRA**

Chisankho ndi mbali imodzi ya chiphunzitso choonadi. Otembenuka mtima akuyenera kupita patsogolo kuposera kupanga chisankho chokhala membala ochitachita ku Thupi la Kristu, kukhala munthu amene angatembenezeso anthu ena. Kupindula anthu atsopano ndichithu chofunikira kwambiri, koma kuphunzitsa anthu kusatira Yesu komanso kukhala anthu obala zipatso ndikofunikira kwambiri. Wina aliyense mutakamuphunzitse akuyenera kukatembenuza anthu, kuwaphunzitsa ndikutitso akathe kufikira anthu ena. Iyi ndi dongosolo yamu Baibulo limene linawoneseredwa ndi Yesu Khristu. Anasakha anthu 12, kuwapanga kukhala ophunzira kenako kuwaphunzitsa kuti akafikire anthu ena.

Chinthudzi ichi chikuonetsa mene mkombero wa uvangeli ndi wophunzira umayendera:



Uvangeli umabwera khonsa zatsopano. Kuphunzitsa kumabala ophunzira amene amatha kukalalikira, ndikukabwera nkhoa za tsopano ndikuwaphunitsaso. Umutu ndimene zimayendera mobwereza bwereza choncho.

### **KUYENDERA MWACHANGU**

Nthawi yomweyo patangochitika kutembenuka mtima, obabwa mwatsopano apasidwe malamulo mumadera awa:

#### **KUTSIMIKIDZIKA:**

Athandizireni kuti akakhale ndikutsimikidzika mtima zachipulumutso chawo komanso kulimba mtima muubale wawo ndi Yesu Kristu.

#### **KUVOMEREDZA YESU PAGULU:**

Alimbikitseni kuti aziperekera umboni za chipulumutso chawo ndiwokhulupirira wina, achibale kapena azawo. Kulankhula ndimbali yofunikira kwambiri mu moyo wachi khristu:

**Kuti ngati udzavomereza m’kamwa mwako Yesu ndiye Ambuye, ndi kukhulupirira mumtima mwako kuti Mulungu anamuukitsa Kwa akufa, udzapulumuka.**

**Pakuti ndi mtima munthu akhulupira kutengapo chilungamo; ndi m’kamwa abvomereza kutenga cipulumutso. (Aroma 10:9-10)**

#### **ABATIZENI NDI MADZI:**

Mu bukhu la Machitidwe, obadwaso mwatsopano amabatizidwa mu madzi pamene amalidza kulandira Yesu Khristu. Malemba pa Machitidwe 8, 9 ndi 16 anawonesera izi. Kufunika kwa ubatizo wa madzi unafotokodzeredwa mu Harvestime International Institute phunziro loti “*Madziko a chikhulupiriro.*”

#### **UBATIZO WA MZIMU WOYERA**

Bukhu la Macitidwe linapereka zitsanzo za momwe otembenuka mtima amalandirira ubatizo wa Mzimu Woyera pakutha kwa uthenga. Onani Machitidwe 8:14-17; Machitidwe 19:1-6. Ubatizo wa Mzimu Woyera unafotokodzeredwa bwino mu Harvestime International Institute phunziro loti “*Utumiki wa Mzimu Woyera.*”



## **KUKHALA MOYO OZIPEREKA:**

Obadwa mwatsopano akuyenera kulimbikitsidwa kuti ayambe kuwerenga Baibulo komanso azipemphera tsiku ndi tsiku. Aphunzitseni ndondomeko ya pephero la Ambuye (Luka 11:1-4) ndikuwalimbitsa kuti aziwerenga bukhu la Yohane.

## **KUKHALA MEMBALA WA MPINGO WA DERA LAWO:**

Ndichofunikira kwambiri kuti onse obadwa mwatsopano akakhale membala wa mpingo omwe uli mu dera lawo ndikuyanjana ndi azawo (Ahebri 10:25). Pamene mukuphunzitsa otembenuka kumene, simukuyenera kukhala ngati ndinu abusa. Mulungu anayika azibusa mipingo kuti akathandizire anthu mu moyo wawo wa uzimu tsiku ndi tsiku. Okhulupirira aliyense akuyenera kukhala pansu pa m'busa.

Athanizireni obadwa mwatsopano kupita ku kachisi. Ziperekeni kuti muziwapasa mayendedwe a galimoto kapena muziyenda nawo kupita ku kachisi. Awoneseni kwa anthu akupingoko ndipo muwonetsetse kuti akutenga nawo gawo ku maphunziro a Baibulo ndi gulu lama pemphero.

Kumbukirani kuti kuyendera anthu mwachangu ndiku SAWASIYA omwe atembenuka kufikira atakhazikika mipingo yawo. Ngati kulibe mpingo, ndiye kuti umodzi ukuenera kukhazikidwa. Gawo Lachitatu yaphunziroli ikuthandizirani kuchita izi.

## **KUKUZA MMENE MUNGAYENDERE**

Pakuphunzira ubale wa Yesu ndi omusatira ake, malamulo ambiri a kuphunzitsa anawoneseredwa. Izi ndizofunikira pakupitiriza mene mungayendere otembuka watsopano:

### **1. KUSANKHA**

Otembenuka mtima aliyense akuyenera kuphunzitsadwa ndi munthu mowirikidza, koma simungakwanitse kuphunzitsa aliyense. Mulipo nokha komanso simuli oyenera kuphunzitsa anthu ambiri pakamodzi. Yesu amasakha anthu amene anawaphunzitsa mowirikidza. Ena amauidwa kubwerera m'makwawo, kumudzi kapena kuzipembedzo zawo.

Mukuyenera kuyetsesa kuwayendera anthuwa mwachangu, koma simungakwanitse kuyendera mowirikidza munthu aliyense mwamutembenuka mtima. Ichi ndichifukwa chake ziphunzitsa zikuenera kuachitikira ku mipingo yamudera lawo. Abusa akawonetsetse kuti otembenuka mtima atsopano akuphunzitsidwa bwino bwino ndi anthu okhwima mu uzimu.

Apemphererani amene mukuwaphunzitsa mowirikidza. Pemphererani amene apita kwa abusa kapena kwa okhulupirira ena mu mumpingo amene akufuna maphunziro. Ngati muli ndi phatso ya utsogoleri okhala olalikira, simuyenera kukhala malo amodzi kuti mukakawaniritse kuyenedera omwe atembenuka kumene. Mukuenera kusakha abusa kapena atsogoleri kuti akamalidzitse ntchito imeneyi.

### **2. KUKHALA NDI ANTHU:**

Pamene Yesu anawayitana ophunzira ake, anawayitana kuti akakhale ndi iye. Anagawana nawo za momwe moyo wake utakhalire. Anakhala nayo limodzi munyengo za kulalikira ndi nyengo zowawa.

Kuphunzitsa sikungachitike kudzera mumikumano ya gulu kapena kupemphera kwa pasabata kokha. Mukuenera kukhala chifupi ndi omwe mukuwaphunzitsawo. Mukuenera kugawana nawo za moyo wanu.

### 3. KUKONZEKERESA

Pakukhala pamondzi ndi Yesu, kuwakozekekesa kunayambika. Yesu anawayitana ophunzira ake kuti akakonzekekesa ku utumiki. Kukodzekekesa uku kumafunika kuvera kwambiri Mawu a Mulungu ndi cholinga chake. (onani Yohane 4:34; 5:30; 15:10; 17:4 ndi Luka 22:42). Musapange ophunzira kudalira inu. Apangeni kuti akadalire pa Mulungu munjira yowakozekekesa.

### 4. MASOPHENYA

Yesu anawalimbitsa omusatira ake powapatsa masophenya a uzimu. Anawayitana ku utumiki waukulu yoponsa moyo wawo watsiku ndi tsiku. Anawayitana omusatira ake kuti akakhale asodzi a Anthu (Mateyu 4:19). Anawapatsa masophenya okolola dziko lonse (Yohane 4:35). Anawatsimikidzira ndi vumulutso la Ufumu wa Mulungu (Mateyu 13).

Popanda masophenya, anthu amawonongeka (Miyambo 29:18). Alibe chitsogodzo komanso kulimbikitsika. Pakuphunzisa muyenera kuwaudza za masophenya awuzimu kuti zikawape kulimbika ku ntchito ya Mulungu. Phunziro la The Harvestime International Institute yoti “*njira zomwetera muzimu ndi kukula maganizo a baibulo*,” zikuthandizirani mene mungakulire mu masophenya awuzimu ngati odabwa mwatsopano.

### 5. MALAMULO:

Pamene mukukuza mene mungawayenderere otembenuka mtima mukuenera kuwauza malamulo onse amene Yesu anapereka. Choyamba, alandire malamulo muziphunzitso za chinkhulupiriro cha a khristu. The harvestime International Institute “*Madziko a chikhulupiriro*” ndiwothandiza mu ntchito iyi. Muli malamulo omwe ali mu Ahebri 6:1-3 omwe ndi:

- Kusiyana nazo ntchito zakufa.
- Chikhulupiriro cha pa Mulungu.
- Chiphunzitso cha ubatizo.
- Kuika manja.
- Kuika kwa akufa
- Chiweruziro chosatha.

Pakusatira maphunzira mumadera awa, ophunzira aphunzitsidwe “*Kukhala mu Ufumu wa Mulungu*,” “*Kulalikira wa Mzimu Woyera*,” “*Kudziwa liwu la Mulungu*,” “*Nkhondo za Uzimu*,” “*Njira zowerengera baibulo*,” ndi “*Kufufuza Baibulo*.” Maphunziro osewa ali mu Gawo Lachiwiri la The Harvestime International Institute.

Cholinga cha malamulo ndikuwabweretsa ophunzira kuti akhale angwiro. Kukhala angwiro zikutanthaunza kuti kukula muuzimu chimere chiri “*kutha, kumalidzika ndi kukula*.” Khristu wa ngwiro ndi amene wafika pa kukula muuzimu, kubweretsa nthupi lake, moyo ndi mzimu

pansi pa ulamuliro wa Mzimu Woyera. Mawu oti “ungwiro” amafanana ndi mawu oti “kusinthika” kapena “kuyeretsa”, amene amagwiritsidwa mu Baibulo, “kusinthika” kumatathaunza chiyero ndi “kuyeretsedwa” kumatanthauza kuti kupatulidwa muchirungamo.

Pali magawo awiri aungwiro:

-Ungwiro wa aliynse, kutanthaunza kuti kukhululukidwa kwa machimo kudzera mu chipulumutso.

-Kukula mu ungwiro, ndinjira yomwe imachita mowirikidza pamene ukusitha kukhala chithunzi cha Kristu. Izi zawoneseredwa mu Aroma 7-8, Afilipi 3:12; 1 Yohane 1:8-9.

## 6. **KUWONETSERA:**

Yesu sanangophunzitsa kudzera mawu amalamulo okha. Anawonetsera zomwe amaphunzitsa. Anaphunzitsa machiritso ndikuwonetsera machiritso pakuchidza odwala. Anaphunzitsa ulamulo wa okhulupirira pa Satana ndipo anawonetsera pakutulutsa ziwanda. Anaphunzitsa zokhuzana osauka ndipo anawonetsera pakudyetsa nkhamu la anthu.

Ophunzira sanala otsatira chabe, analiso mboni pakuwonetseredwa mphamvu ya Mulungu. Pamapeto pake anati amaphunzitsa “Cimene tidaciona m’maso mwathu, cimene tidacipenyenera” (1 Yohane 1:1). Yesu anawonetseraso chiphunzitsa chake ndimene amakhalira moyo wake.

**Pakuti ndakupatsani inu citsanzo, kuti, monga Ine ndakucitirani inu, inunso mucite. (Yohane 13:15)**

## 7. **KUTENGA NAWO GAWO:**

Chidziwitso chongava sichokwanira. Kukhala ochita chita, chidziwitso chikuyenera kugwira ntchito. Ophunzira sanangomvetsera ziphunzitsa za Yesu ndikuwonerera kuwoneseredwa phamvu, koma anatenga nawo gawo. Kuphunzira phunziro sizokwanira. Kuphunzira kokha kuli ngati kuyesera kuphunzira mene mungakodzere ubongo powerenga bukhu. Ophunzira akuyenera kukhala ndi chithudzithudzi chazomwe akuphunzira. Akuyenera kuphunzira mene angagawire Uthenga Wabwino, mene angapepherere odwala, mene angachosere ziwanda ndizina zambiri. Yesu anapereka mwayi oterewu kwa ophunzira ake. Werengani Marko 6:7-13 ndi Luka 9:1-6. Yesu anawatuma ophunzira ake kuti akachite zomwe anawaphunzitsa. Muonetsetse kuti ophunzira anu akakhale ochita mawu otsati okungomva chabe.

## 8. **KUTSOGOLERA**

Pamene ophunzira a Yesu atabwerera kuchokera ku kulalikira, Yesu anayamikira ntchito yawo (Luka 9:10). Mumaphunziro awo onse Yesu anawatsogolera ophunzira ake. Sanawasiye okha muzowawa zawo. Anali nawo kuwakodza, kuwatsutsa ndikuwalimbikitsa. Ophunzira anakumana ndizokhumudwitsa ndizophinja, mukuyenera kuwakozekeketsa mene akakumane nadzo.

## 9. **KUTUMIDZA**

Gawo lomalidza la ophunzira linali pamene Yesu anawatuma ophunzira ake kuti akakhale ophunzitsa anzawo. Anawapatsa ntchito ya kuchulukitsa muuzimu ku kumayiko wonse. Phunziro la Gawo Lachiwiri la Harvestime International Institute likuthandidzirani

pakuphunzisa ophunzira anu kachulukitsidwe ka uzimu. Gawo lachinayi ndi lachisano iwawonetsera mene angapangire ndikupedza zinthu zomwe zingawakudze. Gwiritsani phunziro iri powaphunzitsa mu kulalikira.

### **CHOWONADI CHA KUPHUNZITSA**

Chowonadi cha kuphunzitsa ndichimene chimachitika pamene inuyo simuli pamodzi ndi amene munawaphunzitsa. Kodi akakhalabe okhulupirika kudzomwe munawaphunzitsa? Kodi amalalikirabe ndi kupedza otembenuka atsopano ndiku Wa phunzitsa? Ngati zili chocho, kuyendera kukuchitikadi moyenera:

**Wophunzira sapos a mphunzitsi Wace; koma yense, m'mene atafotokonedwa mtima, adzafanana ndi mphunzitsi Wace. (Luka 6:40)**

## MAFUNSO OZIFUSA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera.

---

---

---

2. Kodi mawu oti “otembenuka” akutanthauzanji?

---

---

---

3. Tanthauzirani “wophunzira”

---

---

---

4. Lembani magawo asanu ndi imodzi a malamulo akuyendera otembenuka mtima otsopano.

---

---

---

5. Perekani mfundo zophunzira zisanu ndi zinai zomwe zikuvumbulutsidwa pa ku phunzira Yesu ndi ophunzira ake.

---

---

---

---

---

6. Chowonadi cha kuphunzitsa ndichani?

---

---

---

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

## ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. 1 Atesalonika 1:2-9 likufotokoza ubwino omwe umadza kamba koyendera kwa bwino. Cholinga ndi anthu amene mukufuna kuwafikira pamene alandira Yesu zanedwa mu 1 Atesalonika 1:9.
2. Ganizani kuyamba “kutenga mu uzimu” pangazi izi mpingo wanu pomwe okhulupirira atsopano akuikidwa panse pa mamembala a mpingo
3. Pali njira zambiri zomwe Paulo amagwiritsa ntchito poyendera anthu:

-Ndimakalata:	1 Atesalonika 1:1
-Ndimapemphero:	1 Atesalonika 1:2; 3:10
-Kutumidza nthumwi:	1 Atesalonika 3:1-5
-kukumana ndi munthu	1 Atesalonika 2:18

4. Pali zizindikiro zambiri za ophunzira a Yesu poganidzira bvumbulutso leni leni pa Mawu a Mulungu, koma khazikikana pa zizindikiro khumi ndi zinayi. Ophunzira ayenera kuchita izi:

(1) Kusiya zonse:	Luka 14:33
(2) Kuzikaniza wekha:	Mateyu 16:24; Luka 14:27
(3) Kutsata Yesu:	Mateyu 16:24
(4) Kufuna Ufumu wa Mulungu:	Mateyu 6:31,33
(5) Kuwonetsera chikondi cha Mulungu:	Yohane 13:34-35
(6) Kukhala mu Mawu:	Yohane 8:31
(7) Ndiwomvera:	Yohane 8:31
(8) Ndikapolo:	Mateyu 10:25; 20:26-28
(9) Kulemkedza Mulungu pakubala zipatso:	Yohane 15:8

5. Werengani Luka 9:57-62 mu Baibulo lanu. Mu nkhanayi, amuna atatu anamupedza Yesu ndicholinga chofuna kukhala ophunzira ake. Kwa wana aliyense wa iwo, Yesu anawonetsera zolinga zosiyana zimene kuphunzira kumafunikira:

### **Lingalirirani cholowa: Luka 9:57-58**

Munthu oyamba amatha kusata Yesu popanda kuyembekedzera kuyitanidwa. Amayetsera kukhala ophunzira wa Yesu kudzera mu mphamvu zake. Yesu anati “Ukanditsata ine, uzakumana ndi izi.” Afotokodzereni kuti kuphunzira kwa chowoonadi kuli ndicholowa chake. Sizimatengera phamvu za munthuu.

### **Zokhumba zeni zeni: Luka 9:59-60**

Munthu wachiwiri amayitanidwa ndi Yesu kuti amutsate. Ku “Sata” kukutanthaunza kuti kubwera pambuyo pa amene wabwera koyamba, kutsata chitsanzo. Zimafuna zonse monga kukhulupirira ndi kumvera. Ophunzira akuyenera kusiya moyo wake wakale chifukwa

chamayitanidwe okha. Zisankho ndi malekano ndi zoperekeka ngati nsembe zikuyenera kukhala zosaziwika ku gulu la anthu. Osatira amasiya moyo otetedzeka ndikusata moyo otsatetedzeka pamaso pa dziko. Kuzipereka uku si pologalamu, koma kwa munthu. Munthu amene ali Ambuye Yesu Kristu.

Bukhu la Luka, mayakhidwe amunthu uyu pakusata Yesu anali “ndisate ine...” Amafuna kusata Yesu koma sichinali cholinga chake. Yesu sananene kuti omusatira otaye zokhumba zamakolo ake (Yohane 19:25-27). Munkhaniyi akukamba za zokhumba zeni zeni. Munthu uyu amafuna akayike kaye bambo ake mmmanda. Panthawi yovuta imene Yesu akumuyitana munthu kuti amutsate, pasakhale chinthu chomwe chikayikidwe kuyakho lanu.

Kusatira Yesu siizikutanthaunza kuti ophunzira aliyense akasiye nthito zawo kapena mabanja awo. Zimene zikutanthaunza ndizoti zimafunikira kuti mankhalidwe amunthu akuyenera kusitha. Nthawi zina zimathaunzatsa kuti mukasiye mabanja anu, ntchito zanu komanso okonedwa chifukwa cha Uthenga Wabwino. Mukuyenera kupita kulikonse komwe Yesu akukupitisanu. Kuphunzira chikakhale cholinga.

### **Zolinga zeni zeni: Luka 9:61-62**

Munthu wachitatu mu Luka 9:57-62 amafuna amusate, koma amafuna kuchita mumalamulo ake. Kukasadzika azibale ake chinali chinthu choyenera kuchita, koma Yesu wamuyitana. Cholinga cheni cheni chinali chani mumoyo wake? Kuphunzitsidwa kapena kuchita zinthu zake? Zolinga zamunthuyu mumoyo wake zinali zosakhazikika. Amaziletsa, anali pakati pamoyo wake wakela ndiwatsopano omwe Yesu anamuyitana.

6. Umu ndimomwe mungachitire pakuyendera anthu obadwa mwatsopano, pali magawo atatu:

### **Nkumano Woyamba: (Ikachitike mumawola 24 mutamalidza zokambirana zanu)**

\_\_\_ Ayimbileni otembenuka atsopanowo ndikupedza malo oti mukumane ndi nthawi yokumana.

\_\_\_ Pankumano oyamba, funani kuti mukhazikitse ubale omasuka ndi chimzake. Alore ni aziwe mmene angakupedzereni mwina pamene ali ndimafunso ndi zankumano wanu.

\_\_\_ Afunseni ngati ali ndi mafunso ndipo muyesere kuyawankha.

\_\_\_ Yambani kuwatsogolera mumadera akuyendera mwachangu omwe ali mu muphunziro iyi amene ndi:

- Kusimikidza ku Chipulumutso
- Ubatidzo wa Mzimu Woyera
- Kuvomeredza Yesu pagulu
- Kukhala moyo odzipereka ku mawu
- Ubatidzo wa madzi
- Kukhala membala wa mpingo

\_\_\_ Muwasiyire bukhu la Harvestime International Institute, aphunzire “*Madziko a Chikhulupiriro*,” alimbikitseni kuti awerenge phunziro loyamba.

\_\_\_ Pempherani Limodzi

\_\_\_ Pangani nthawi ndi malo ankumano wina.

**Nkumano Wachiwiri: (Ikachitike patatha sabata)**

\_\_\_ Onani Phunziro Loyamba mu “*Madziko a Chikhulupiro*”

\_\_\_ Funsani ngati ali ndi mafunso ndipo yenserani kuwayankha.

\_\_\_ Apaseni Phunziro Lachiwiri la “*Madziko a Chinkhulupiro*”

\_\_\_ Pitiridzani kuwatsogolera mu magawo 6 amene anenedwa mu “kuyendera mwachangu”

\_\_\_ Afunseni ngati ali ndi zovuta zina kapena zokayikira

\_\_\_ Pepherani limodzi, pephererani zomwe mwakambirana.

(Mikumano yosalayi muzakambirane pakutha sabata imodzi.)

**Nkumano Wachitatu:**

\_\_\_ Onani phunziro lachiwiri mu “*Madziko a Chikhulupiro*” limodzi.

\_\_\_ Afunseni ngati ali ndi mafunso ndipo muyesere kuwayankha.

\_\_\_ Apaseni phunziro lachitatu wamu “*Madziko a Chinkhulupiro*”

\_\_\_ Pitiridzani kuwatsogolera mu magawo 6 amene anenedwa mu “*kuyendera mwachangu*”

\_\_\_ Afunseni ngati ali ndi zovuta zina kapena zokayikira

\_\_\_ Pempherani limodzi, pemphererani zomwe mwakambirana.

(Mikumano yosalayo mutha kuchita monga mwachitita ndi nkumano 3. Pakutha pa miyedzi itatu, onana mene akuchitira pa magawo 6 omwe alembedwa mu “kuyendera mwachangu”).



## CHAPUTALA 14

### KUKONZEKERA UVANGELI

#### ZOLINGA:

- Kulemba vesi yotsogolera.
- Kufotokoza phindu lokonzekera
- Kufotokoza chifukwa chani kukonzekera kuli m’Baibulo
- Kugwiritsa satane satane wokonzekera waperekedwa mu phunziro ili za kulalikira.

#### VESI YAPA MTIMA:

**Mzimu wa Ambuye uli pa Ine, Cifukwa cace Iye anandidzoza, Ine ndiuze anthu osauka Uthenga Wabwino; Anandituma Ine kulalikira am’singa mamasulidwe, Ndi akhungu kuti apenyenso, Kuturutsa ndi ufuru opwanyika. (Luka 4:18)**

#### CHIYAMBI

Mu bukhu la Macitidwe muli njira ziwiri zazikulu zomwe mpingo woyambirira umagwiritsa ntchito polalikira ku dziko lonse zomwe ziri zofunikira lero lino. Uvangelis oyamba, unali pamene okhulupirira amavomeredza mwachangu mwayi ndi mwansangansanga kugawa Uthenga Wabwino. Chachiwiri ndikukodzekera njira za uvangeli. Maulendo a utumiki a Paulo ndi kubzala mipingo ndi umboni oti amakodzekera.

Okhulupirira onse akuyenera kukhala atcheru kumwayi wolalikira mpopompopo, koma kukodzekera kukalalikira ndi njira yomwe mukuyenera kutenga mwadaladala. Muphunziro iyi mukhaphunzira mene mungakodzekerere uvangelis.

#### KUKODZEKERA KUKOLOLA MUUZIMU

Kukodzekera kuli ngati ulimi. Mulimi antha kulima tiligu kummawa kwa United States, ma olenji ku Israyeli, ndi mpunga ku Afilipo.

Mumadera onsewa muli zinthu zofanana: mbewu zimalimidwa ndipo pali zinthu zofanafana ngati dothi, chonde, mbeu, madzi, kuunika, matenda, tidzilombo ndi zogwirira ntchito. Koma ulimi ndiwosiyana potengera mbewu zomwe zalimidwa, dera ndi kupezeka kwa zinthu zaluso.

Chimodzimodzi muzokolola za uzimu. Simungapange uvangeli pa okha kuposera mulimi angapangire ulimi pa okha. Ngati mukufuna kukapindura, mukuyenera kukhala ndi dongosolo lowoneka, zolinga, njira ndi kusatira ntchito. Mukuenera kuziwa cholinga chanu ndi dongosolo kuti mukakwaniritse cholinga.

#### PHINDU LA KUKONZEKERA

Kukodzekera kumakuthandizirani kuti mukakhale wa ntchito wa dzeru ku Uthenga Wabwino ndi zida zochitira kulalikira ngati zomanga, katundu, zida za magesi, zachuma, ndi mphatso za Uzimu za okhulupirira omwe mukuwayang’anira. Kukodzekera kumapereka chitsogodzo, kumakuthandizira kuti mukapange zitsakho zabwino, kuzakitsa zolinga za kulalikira, zikupangitsani inu kuziwa pakuwokhesa. Zimakulolani inu kuchita zinthu mwadzeru kuposa kukachita zinthu molakwikwa.

## KUKONZEKERA NDI KWA BAIBULO

Baibulo lazadzidwa ndi nkhani za amuna ndi akadzi omwe anapanga dongosolo pakutsogozedwa ndi Mulungu. Yona anapanga dongosolo lokodza chombo. Abulahamu anayika zolinga kwa kapolo wake, Elieza (Genesis 24). Yosefe anakonzekera zaka zonse za njala (Genesis 41). Mose anapatsidwa dongosolo lokatulutsa a Isirayeri ku ukapolo ndi kuti akamange kachisi. Yoswa anapanga dongosolo lokagonjetsa dziko lamalonjedzano.

Davide anakonzekera kumanga kachisi. Mfumu Hezekiya anali nalo dongosolo yoyeretsa Isirayeli, ndiponso Nehemiya anali nalo dongosolo lokamanganso Linga. Chipangano chakale aneneri amawonetsera dongosolo la Mulungu lomwe wayika ku dziko, ndipo mu bukhu la Cibvumbulutso likuwonesha dongosolola Mulungu lamutsogolo.

Anthu ena amakhulupirira kuti kukonzekera kuma tchinga ufulu wa Mzimu Woyera, koma izi sizoon. Mzimu woyera atangotsika pa Macitidwe 2, pakutha pakanthawi yochepe kukonzekera kunayambika pakutsogozedwa ndi Mzimu Woyera (Macitidwe 6). Zozizwa zomwe zinachitika ku mpingo oyamba zikuwonetsera kuti kukonzekera sikunasokonedze ntchito ya Mzimu Woyera!

Kukonzekera kutha kukhala pakulambira, nthawi imene mumawona cholinga cha Mulungu ndi kupanga dongosolo ndipamene mumatsegula mzimu kuti akutsogorereni. Pamene mukupephera ndiku werenga Mawu a Mulungu ndikupanga dongosolo ndikukhuzika kwa Mzimu Woyera, kukonzekera ndintchito ya Uzimu. Kukonzekera sikutchinga koma kumagwiridzana ndi Mulungu. Chitsanzo chimodzi cha dongosolo ndi Yoswa pa Ai (Yoswa 8). Anali ndi dongosolo (vesi 4) koma sinatchinge zozizwa za Mulungu (vesi 18). Dongosolo laku thupi ndi zochitika zauzimu zimagwira ntchito limodzi, paumodzi kukwaniritsa cholingacho.

Yesu anapanga dongosolo la utimiki. Anakonzekera kukalalikira Uthenga Wabwino, kuchilitsa odwala, kutulutsa ziwanda, ndikukapanga zozizwa kutsimikidza Mawu a Mulungu. Anakwaniritsa cholinga cha Mulungu pakufera machimo amitundu yonse ya anthu, kukawononga ntchito za oyipa, kukawuka kwa akufa ndimphamvu ndi ulemmero. Yesu anati:

**Mzimu wa Ambuye uli pa Ine, Cifukwa cace Iye anandidzoza, Ine ndiuzo anthu osauka Uthenga Wabwino; Anandituma Ine kulalikira am'singa mamasulidwe, Ndi akhungu kuti apenyenso, Kuturutsa ndi ufuru opwanyika. (Luka 4:18)**

Paulo anapanga madongosolo, apo ayi Mzimu Woyera siwukanawasitha ndimmne zaonetsedwera pa Macitidwe 16:6-10. Yesu anawapasa dongosolo la uvangeli mu Macitidwe 1:8. Pamene tikupanga dongosolo la uvangeli tikungolemba momwe zitakhalire.

## DONGOSOLO NDI CHANI?

Mfundo iri yonse yomwe idzachitike kutsogolo ndi mfundo ya chikhulupiriro. Dongosolo ndi mfundo za chikhulupiriro. Kusapanga mfundo iri yonse yakutsogolo ndikukhala opanda chikhulupiriro.

Dongosolo ndi njira imene imakuthandidzirani mmene mungafikire ku zokhumba zau za uvangeli. Kukonzekera kumakukakhirani inuyo kuti mukafune malingaliro a Mulungu ndi cholinga cha Mzimu Woyera. Kodi Mulungu amakhumba chani? Kukonzekera

kumakuthandizani kuti mukadziwe zithu zomwe simungachite, poti chimachosamo zithu zina.

Phunziro la The Harvestime International Institute, la “*Kusamaliidwe ndi zolinga,*” likunthandizani pamene mukukodzekera. Kumbukirani nthawi zonse, pena—muntha kutaya nthawi yanu pa moyo kufufudza ndikupanga dongosolo koma otsapeza chinthu cheni cheni chomwe chinakupangitsani kuti mufufunze. Ndikufufuza ndi kupanga dongosolo la uvangeli, osati kungopanga basi opanda zolinga.

### **MITUNDU YAKUKONZEKERA**

Mitundu imayamba pongoganidzira kuti sitikudziwa zofuna za Mulungu pa anthu ena. Dzimathandizira kuti tiyike pambali madongosolo omwe tinali nawo komanso zomwe timaganidza ndikumulola Mzimu Woyera kutsogolera. Iyi ndi mitundu ya kukodzekera:

#### **FOTOKODZANI KUTI NTCHITO NDICHANI:**

Kututa kwakukulu kwa uzimu tikuyenera kukolola kuli mminda yambiri kumayiko osiyanasiyana. Mukuyenera kuziwa kuti ntchito yanu ndichani. Kodi mukufuna kukalalikira ndani? Amakhala kuti? Ndi anthu otani? Mukuyenera kufotokadza za kututa munda mumagawo awa: mmene deralo liliri, chikhalidwe ndi chilankhulo. Phunziro la Harvestime International Institute la “*kudziwa madera*” ikuthandizani kwambiri.

#### **PEDZANI NJIRA ZA BWINO ZA UVANGELI:**

Pali njira zambiri za momwe mungatumikirire zomwe zanenedwa muphunziro ili. Pazimene mwaphunzira pomwe mukufuna kuziwa ntchito yanu, kupemphera kwambiri kumakuwonetserani njira za bwino za uvangeli. Ndizofunikira kwambiri kuchita izi chifukwa simudzataya mphamvu zanu pachabe. Mwachitsanzo, uvangeli wapakanema sukupindula ngati anthu amuderalo alibe makanema. Uvangeli wolembedwa m’*mabuku* sukupindula ngati anthuwo ndiwosaphunzira. Kumbukirani kuti njira yomwe mutagwiritse ntchito ikakuwonetserani zomwe simukachita bwino ndizome mukachitetso.

#### **PEDZANI NJIRA ZA UVANGELI:**

Muli ndi njira ziti zopangira uvangeli? Mukagwiritsa ndani pokalalikira kwa gulu la anthu kapena deralo? Ndi zachuma zingati zomwe muli nadzo? Mukafuna zida zANJI (zida za magesi, mathalakiti, ndizina zambiri).

#### **PANGANI DONGOSOLO LA KULALIKIRA:**

Dongosolo lanu likakhazikike pa uvangeli osati pakutukuka. Mukakhazikike pa kukudza Ufumu wa Mulungu, osati malamulo a mipingo kapena mabungwe. Mudongosolo mukakhale zolinga zomwe ziri mfundo za zokhumba zomwe mukufuna kukakwaniritsa. Mundo zikakhale:

-Zikalembedwe

-Zokhuzana ndi uvangeli

-Zikafotokodzeredwe bwino.

-Mukafanizire chikhulupiriro ndi zenizeni.

-Mukhale otsimikidza: madongosolo osamvetsetseka ndiwovuta kuwachita. Dongosolo lano mukayikemo mfundo zoti uyu akachita izi ndi ndani kufikira pakuti ndi mene zitakachitikire.

-Mukhale owonetsetsa: mukawonetsetse kuti dongosolo liri lonse yakwaniridwa.

-Mukakhale utsunga nthawi: magawo ena a dongosolo akuyenera kuchita pamene ena asanamalidzike. Zolinga zina zofunikira kuposa zina.

### **KUCHITA DONGOSOLO PA UVANGELI:**

Kupanga dongosolo kokha sikukwaniritsa ntchito ya uvangeli. Mukuyenera kugwiritsa ntchito dongosolo. Kugwiritsa ntchito dongosolo zikuthanthauza kuti ikatsatiridwe. Kugwiritsa ntchito dongosolo ili motere:

- Sankhani anthu omwe akakwaniritse dongosolo.
- Auwauzeni za dongosolo anthuwo.
- Kaperekani maudindo kumagawo otsiyanatsiyana a dongosolo.
- Phunzitsani anthu kuti akagwire ntchito.
- Kbweretseni pamodzi anthu, katundu, zochitika.
- Kuyika matsiku azochitika.
- Kupanga dongosolo la zachuma.
- Kupanga ziganidzo.
- Kuwona ngati mukupita potsogolo.
- kuwona zotsatira.

### **KUWUNIKIRA DONGOSOLO LA UVANGELI**

Pamene mukuwunikira chinthu muma chifufuza bwino ndikuona ubwino wake. Kuwunikira ndi njira yomwe mumaona ma dongosolo ndikuwona ubwino wake pakupindula pacholinga cha uvangeli. Zolinga zimanena madongosolo omwe mukufuna kuchita. Kuwunikira kumakuwonetsani ngati mwakwaniritsa zolinga zanu. Ngakhale Mulungu anawunikira ntchito yake mu Genesis 1. Anayendera zonse zomwe analenge ndipo anati, “Ziri bwino.” Kuwunikira kutha kukuonetsani kuti mukawonetso bwino zolinga zanu, mukasinthe mwa anthu omwe akugwira ntchito pazolinga, mukasinthe matsiku okutha kale, mukasinthe njira, kapena mukasinthe zachuma zanu. Pamene mwamalidza ma dongosolo anu, wunikirani poyankha mafunso awa:

- Mwafikira cholinga chanu?
- Mwalephera pati? Chifukwa ndi bwanji?
- Mwakwaniritsa pati? Chifukwa ndi bwanji?
- Mukanapanga mosiyana bwanji? Njira dzina, anthu ndi dongosolo?
- Kodi chuma cha anthu, zinthu zogwiritsira ntchito ndi ndalama zinagwiritsidwa ntchito bwino?
- Mudzagwiritsatso ntchito dongosolo?
- Mungaphunzire chani kuchokera ku izi zomwe zingakuthandizani popanga dongosolo lina?

...kenako kagwiritseni ntchito zomwe mwaphunzira kuti mukayambenso mkombero wa uvangeli.

## MAFUNSO OZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera.

---

---

---

2. Fotokozani phindu la kukonzekera.

---

---

---

---

3. Fotokozani chifukwa chimene kukonzekera kuli m’Baibulo.

---

---

---

---

---

---

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

## ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Popitiridza maphunziro anu pa kukonzekera, pezani phunziro la The Haverstime International Institute, “*Kusamalidwa ndi zolinga*”
2. Perekani mfundu zomwe zaperekedwa mu chaputala ichi pakupanga dongosolo la uvangeli mu dera lanu.
3. Kuchita dongosolo laphamvu la uvangeli pamafunikira zinthu zambiri monga mikumano, kubwera pamodzi, kuthana ndimavuto ndikuwunikira. Sizingatheke kuti tikambe mitundu yonse ya mikumano mikuyenera kuchita, koma pali mmene mungapangire madongosolo kapena mikumano:
  - (1) Mukhale ndicholinga cheni cheni cha nkumano: Chifukwa chani uli ofunikira? Cholinga chanu ndichani? Mukufuna kukwaniritsa chani?
  - (2) Pangati mutu wa nkumano: lembani zinthu zomwe mungazakambirani mwakufunika kwake. Nthawi zonse mukayikepo nthawi yopemphera kufuna chitsogodzo cha Mulungu.
  - (3) Lembani zinthu zonse mukufuna kulakhalanazo pa nkumano: zinthu monga pensulo, pepala, zosatira, zitsanzo ndizina zambiri. Ikani pamodzi zinthu zonse zofunikira kunkumano.
  - (4) Sankhani tsiku, nthawi, ndi malo ankumano.
  - (5) Adziwitseni anthu amene mukufuna kuti abwere kunkumano: apatseni tsiku, nthawi, malo, ndi cholinga cha nkumano. Adziwitseni ngati akuyenera kubweretsa chinthu chirichonse.
  - (6) Yambani ndikumalidza nkumano pa nthawi ya bwino.
  - (7) Sankhani wosogolera kunmano.
  - (8) Nkhalani ndinjira yoyankhulira: anthu azikweza manja ndikuyitanidwa ndi tsogoleri? Kukhala kukambirana kwa gulu?
  - (9) Nkhalani ndi njira yopangira chitsankho: Mupephera pakana onse atamalidza? Kodi azibusa kapena anthu ena otsogolera akapanga chitsankho pakutha kuva zonena za anthu?
  - (10) Nkhazikikani pacholinga: musasokonedzeke ndizokamba dzina.
  - (11) Musunge zonse zakambidwa pa nkumano, kwambiri ponena kuti ndindani atapange chakuti ndipo kufikira liti. Pakutha kumano, mulembetso bwino bwino zomwe mwakambirana ndikumupatsa aliyense anabwera ku nkumano. Izi zikawathandizira kuti akakumbukire ntchito yomwe apatsidwa kuti akagwire.

## CHAPUTALA 15

### KULUMIKIZANA PA UVANGELI

#### ZOLINGA

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba ves yotsogolera
- Kutanthauzira “kulumikizana”
- Kufotokoza mmene mpingo umalumikizanirana
- Kufotokoza Mphamvu za kulumikizana
- Kufotokoza kufunika kwa mphatso za uzimu ndi kulumikizana
- Kufotokoza mgwirizano omwe umadza chifukwa cha kulumikizana
- Kufotokoza mmene kulumikizana kumagwirira ntchito

#### VESI YOTSOGOLERA:

**... akukhala naco cikondi comwe, a moyo umodzi, olingalira mtima umodzi;**

**Musacite kanthu monga mwa cotetana, kapena monga mwa ulemerero wopanda pace, komatu ndi kudzicepetsa mtima, yense ayese anzace omposa iye mwini;**

**Munthu yense asapenyere zace za iye yekha, koma yense apenyereenso za mnzaceo. (Afilipi 2:2-4)**

#### CHIYAMBI

Mwaphunzira kale zambiri za uvangeli mu phunzirori, ndipo mwina kuchuluka kwa ntchito kukukupatsani mantha. Moona mtima ndi ntchito yayikulu.

Koma inu simuli nokha ayi. Muli mbali imodzi ya ogwira ntchito mu munda wa Ambuye. Mu phunziro iri muphunzira ubwino wolumikizana ndi anthu ena pa uvangeli.

#### KULUMIKIZANA

Kulumikizana ndi nchitidwe obweretsa pamodzi m’mbali zosiyana kuti zikhale chinthu chimodzi. Kukamba musavuta, kulumikizana ndi anthu kulakhulana wina ndi m’dzake, kugawana malingaliro, nkhani, ndi chuma ndicholinga chokakwaniritsa cholinga chawo. Kulumikizana kutha kufananizidwa ndi mfundo za ukonde wa nsomba omwe ziri ndi magawo a mlingo wosiyanasiyana, lomwe gawo lina lililonse limalumikizana ndi gawo linzake. Thupinso la munthu nalo ndi lolumakizidwa bwino ndi misempha, minofu ndi magazi. Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera ndi olumikizidwa mwa umulungu.


Tikamakamba za kulumikizana pa uvangeli, timakamba za okhulupirira ena, mipingo, ndi mabungwe achi Khristu pogawana maganizo, nkhani, ndi chuma pofuna kukakwaniras cholinga chimodzi. Palibe mpingo omwe uziganiza kuti uli okha ngati osankhidwa kukhala chida cha Ambuye kukalalikira dziko lonse. Kulumikizana ndi ubale wa pa okhulupirira omwe uli pulani la Mulungu yomwe imaonetsedwera mu Mpingo.

## MPINGO NDI WOLUMIKIZIDWA

Mpingo ndi chitsanzo cha kulumikizidwa. Werengani 1 Akorinto 12:4-31. Mu ndimeyi Mpingo ukuonedwa ngati thupi lomwe liri ndi zigawo zambiri zomwe ziri ndiokhulupirira a mphatso ogwira ntchito limodzi mu utumiki. Monga ngati thupi la munthu, membala wina aliyense wa Thupi la uzimuli ali ndi cholinga. Ndi wogwirizana pa kagwiridwe ka ntchito ndi Thupi lonse. Mphamvu yomwe imatsogorera gwirizano wa Mpingo ndi ulamuliro wa Mawu a Mulungu ndi utsogoreri wa Ambuye Yesu Khristu.


## MPHAMVU YA KULUMIKIZANA

Anthu agwiritsa ntchito zitsanzo zoyisanasiyana pofuna kuwonetsera mgwirizano omwe ulipo ndi anthu ena. Anthu ena agwiritsa ntchito zingwe zolumikizana.




Ngati mungagwire ntchito limodzi ngati zingwe zolumikizana, polumikizana pofooketsetsa pamakhudza chingwe chonse. Polumikizana pofooka patha kupangitsa chingwe kuduka, ndipo kulumikizana ndi ena kumasongonekera.

Anthu ena amagwira ntchito pa kutengera kapangidwe ka piramidi, komwe kamakhala ndi atsogoleri pamwamba, ogwira ntchito pansi:




Kagwiridwe ka ntchito kotereka kali ndi mabvuto ofanana ndi kalumikizidwe ka zingwe. Ngati atsogoreri angalephera, kapena ogwira ntchito omwe ali pansi nawonso kulephera, kagwiridwe ka ntchito kamasokonekera.





Kwa zaka zochuluka, umu ndi mmomwe takhala tikugwirira ntchito ya utumiki. Koma kagwiridwe aka kamapangisa kuti anthu azipikisana osati kugwira ntchito limodzi. Anthu amaponda anzawo ndicholinga choti akafikire pamwamba. Okhulupirira akuyenera kumagwira ntchito ya utumiki molumikizana. Kulumikizana kulibe mabvuto a kugwirizana kwa chingwe ndi piramidi.

Nachi chithunzi cha kagwiridwe ka ntchito molumikizana:



Ingakhale mbali imodzi yalephera kugwira ntchito, mbali zina zimapitiriza kugwirabe ntchito. Kagwiridwe ka ntchito kolumikizana ndikofanana ndi mmene thupi la munthu lomwe likufananizidwa ndi Mpingo. Ngati chala chanu chavulala, zala zina zimabwera kuzathandiza kuti mukafikire mulingo wa ntchito.

Izinso ndi momwe Thupi la Khristu liriri. Pamene mukulumikizana ndi ena pa uvangeli, amapereka mphamvu pomwe inu mukufooka. Inunso mumapereka mphamvu pomwe iwo akufooka. Anthu samapanga mpikisano ndi anthu ena, pakuti pakulumikizapa palibe “pamwamba” poti mukafikepo.

Mukulumikizana, timaika pamodzi chuma chathu ndi cholinga cha uvabgeli. Palibe modzi wa ife amakhala ndi mphatso zonse za uzimu. Patokha, timakhala ndi kuthekera kochepe. Komanso tiri ndi nthawi, zipangizo, ndi chuma chochepe. Koma tonse pamodzi, tiri ndi chuma cha mphamvu kukatuta zokolola za uzimu.

Mphamvu yina ya kulumikizana ndiyakuti nthawi zonse imakula pomwe okhulupirira amakafikira ndikkumanga ma ubale ndi iwo omwe ali kunja kwa Thupi la Khristu ndi kuwabwerensa mu kulumikizana kwa okhulupirira. Mwa ichi, kulumikizana kwa okhulupirira kunka nakulirakulira.

### **MPHATSO ZA UZIMU NDI KULUMIKIZANA**

Aefeso 4:11-16 imabvumbulutsa kuti Mulungu waika mphatso zauzimu zapaderadera mu Mpingo kukakonzekeretsa ma membaka ena ku ntchito ya utumiki. Mphatso zapaderadere za utsogoleri ndi za atumwi, aneneri, avangeli (alaliki), abusa, ndi ena aphunzitsi.

Ntchito ya azitsogorerira ndikukonzekeretsa anthu ku ntchito ya utumiki pakuwathandiza kuti akazindikire ndikugwiritsa ntchito mphatso zawo za uzimu. Mawu oti “kukonzekeretsa” amachokera ku mawu achi Greek omwe amatathauza kuti kuika pamodzi mafupa osweka kapena kubwezeretsa m’ malo mwake fupa losweka. Imakamba kuika pamodzi mbali zosiyana kuti thupi likagwire ntchito bwino. Kulumikizana sikumachosa utsogoleri operekedwa ndi Mulungu. Koma mmalo molekanitsa Thupi la Khristu, ndi udindo wa azitsogolere achi Khristu kuipa pamodzi magulu otsiyansiyana a anthu kuti akakwaniritse cholinga chimodzi chomwe chiri ntchito ya utumiki.

### **KULUMIKIZANA NDI MGWIRIZANO**

Muchilankhulo choyambirira cha Baibulo, mgwirizano umatanthauza “umodzi” mu chi Greek ndi “kuika pamodzi” muchi Aheberi. Mgwirizano ndi mphamvu yayikulu. Muluka anaonga ntchito yaku Babulo chifukwa anadziwa kuti anthu ali pa mgwirizano pa ndi cholinga chimodzi ndipo palibe chomwe chinali chosatheka kwa iwo (Genesis 11).

Chithunzithunzi chabwino ndi mgwirizano wa Mulungu. Yesu anapemphera kuti okhulupirira akhale amodzi, monga Atate analiri mwa iye ndi Iye mwa Atate:

**Kuti onse akakhale amodzi, monga Inu Atate mwa Ine, ndi Ine mwa Inu, kuti iwonso akakhale mwa Ife: kuti dziko lapansi likakhulupire kuti Inu munandituma Ine. (Yohane 17:21)**

Chotsatira cha mgwirizano ndi kukula kwa uvangelu: “kuti dziko likakhulupirire.” Okhulupirira akamalumikizana mwa mgwirizano ndi mayankho a pemphero la Ambuye ndi cholinga cha uvangeli.

Cholinga cha mgwirizano sichingakhale pa ziphunzitso, chifukwa cha katanthauziro kosiyansiyana ka chiphunzitso malingana ndi kusiyana kwa mipingo. Chichingakhalenso pa kulumikizana pa mabungwe chifukwa cha kusiyana kwa ma bungwe achi Khristu. Cholinga ndi mgwirizano wa uzimu omwe umakhazikitsidwa ndi mphamvu ya Mzimu Woyera.

Cholinga cha kulumikizana chikupanga mpingo umodzi okhala pansu pa ulamuliro umodzi, koma ndi gwirizano omwe umafuna kugwira ntchito imodzi kukwakaniritsa chifunira cha Mulungu:

**Anatizindikiritsa ife cinsinsi ca cifuniro cace, monga kunamkomera ndi monga anatsimikiza mtima kale mwa iye.**

**Kuti pa tnakonzedwe a makwaniridwe a nyengozo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Kristu, za kumwamba, ndi za padziko. (Aefeso 1:9-10)**

Ngakhale pali kuyiyana kwa ziphunzitso, onse okhulupirira ali ndi malo mu mgwirizano wa Khristu. Tonse ndife gawo la Thupi la Khrist. Chifukwa cha ichi, tikuyenera kusaka kagwiridwe ka ntchito limodzi:

**...kuti mukalingalire mtima zomwezo, akukhala naco cikondi comwe, a moyo umodzi, olingalira mtima umodzi.**

**Musacite kanthu monga mwa cotetana, kapena monga mwa ulemerero wopanda pace, komatu ndi kudzicepetsa mtima, yense ayese anzace omposa iye mwini.**

**Munthu yense asapenyere zace za iye yekha, koma yense apenyereenso za mnzace. (Afilipi 2:2-4)**

Ndikugwirizana kwathu mwa chikondi komwe kumapangisa dziko kudziwa kuti ndife Akhristu.

**Mwa ici adzazindikira onse kuti muli akuphunzira anga, ngati muli naco cikondano wina ndi mnzace. (Yohane 13:35)**

### **KAGWIRIDWE KA NTCHITO KA KULUMIKIZANA**

Kagwiridwe ka ntchito ka uvangeli zikutanthauza kuti kuika pambali zochita zathu kuti tikagwirizane ndi okhulupirira ena pa kufaritsa Uthenga Wabwino. Ndimagawana maganizo ndi zopeza zathu ndi ena. Timapemphera limodzi ndi kugwira ntchito limodzi pokafikira cholinga chimodzi. Timagawana anthu, mphatso za uzimu, zipangizo, ndi chuma—zonse pa cholinga cha uvangeli.

### **MGWIRIZANO WATSOPANO**

Baibulo limakamba zochitika ziwiri zosiyana zokhuza kugwiritsa ntchito ukonde zomwe zimaonetsera choonadi chachikulu cha uzimu. chochitika choyamba chinachitika kumayambiriro kwa utumikiwa Khristu pa dziko ndipo chinalembedwa pa Luka 5. Ophunzira anakhala akuweza utsiku wonse koma sanakoke kanthu. Yesu anawaudza kuti:

**Kankhira kwa kuya, nimuponye makoka anu kukasodza. (Luka 5:4)**

Peturo anati:

**Ambuye, tinagwiritsa nchito usiku wonse osakola kanthu, koma pa mau anu ndidzaponya makoka. (Luka 5:5)**

Koma pomwe anaponya makoka anazinga unyinjira waukuru wansomba ndipo makoka ao analikung'ambika ndipo anakodolo anzawo a m'ngalawa yinayo kuti awathandize. Nsomba zinali zambiri ndipo anadzaza ngalawa zonse ziwiri, kotero kuti zinalinkumira. Pakuona izi Peturo anadabwitsika koma Yesu anati kwa iye:

**Usaope, kuyambira tsopano udzakhala msodzi wa anthu. (Luka 5:10)**

Nsomba zomwe amagwira matsiku onwe sizinali zoyerekeza ndi kuchuluka kwa kukolola komwe akatute mu dziko la uzimu pomwe anakhala msodzi wa anthu. Chochita china chofanana ndi ichi chinalembedwa pa matsiriziro a utumiki wa Khristu pa Yohane 21. Okhulupirira anaweza utsiku onse koma sanakoke kanthu. Koma pakulamula kwa Khristu anaponya makoka ndipo, anakoka unyinjira wa nsomba. Koma panali kutsiyana ndi nthawi yoyamba ija. Khoka silinang'ambike.

**Cifukwa cace Simoni Petro anakwera m'ngalawa nakokera khoka kumtunda Iodzala ndi nsomba zazikuru, zana limodzi, ndi makumiasanu ndi zitatu; ndipo zingakhale zinacuruka kotere, kokha silinang'ambika. (Yohane 21:11)**

Zochitika ziwiri izi zinachitika mu dziko lakuthupi, koma ziri ndi matanthauzo auzimu. Nthawi yoyamba khoka linang'ambika, koma kachiwiri siyinang'ambike. Kodi chinayisaninsa ndi chani?

Khoka loyamba linali chitsanzo cha kulimbikira kwa munthu. Peturo anali msodi. Amadziwa njira zoonyera khoka ndi zikhalidwe za asodzi. Kudzera mu khoka long'ambika Yesu anamuonetsera kuti kulimbikira kwa munthu kokha sikunngakwanise kukwaniritsa masomphenya ndi ntchito ya Mulungu. Pamene Peturo anadzindikira ntchito yayikulu yomwe Mulungu akumuyitanira, iye analira:

**Koma Simoni Petro, pamene anaona, anagwa panso pa mabondo ace a Yesu, nanena, Mucoke kwa ine, Ambuye, cifukwa ndine munthu wocimwa. (Luka 5:8)**

Peturo anakhala msodzi wa anthu. Kulumikizana kwa kale siikunakakwanisa kusungu zokolola zochulukira za uzimu zomwe angakatute. Peturo amayenera kusiya zikhalidwe za anthu. Amayenera kupitirira malire a Ayuda ndi amitundu. Kulumikizansidwe kakale kamayenera katswedwe ndipo akhale mbali ya kulumikiza kwatspano.

Pakati pa usozi woyamba ndi wachiwiri, mgwirizano watsopano unapangidwa. Zochitika za uzodzizi zinali chiwonetsero cha zinthu zomwe zikuchitika mu uzimu. Mulungu anali akudzutsa mgwirizano watsopano. Omwe ukaphwanye kulekanitsa pakati pa Ayuda ndi amitundu, olemera ndi otsauka, akapolo ndi afulu. Ikakula kuufikira kwa Paulo, Banabasi, Sila, Tito ndi anthu ena ambiri, ndiponso kukafikira kuchokera ku Yerusalemu, kupita ku Yudeya ndi Samaliya, ndikukafikira kumalekezero a dziko.

Utumiki waukulu sungakwaniritsidwe ngati sipangankhara “khoka” mu dziko la uzimu. Mulungu anati mumatsiku otsiriza azatsanurira Mzimu wake pa anthu onse. Aneneri a Chipangano Chakale ananenera kuti mu matsiku otsiriza a zokolola za uzimu nkombero uzakhala waukulu kuti olima azapitirira okulola.

Kukulola kwa uzimuku sikungakololerdwe ndi munthu modzi, bungwe limodzi, kapena mpingo umodzi. Ndichifukwa chake Mulungu anati mumatsiku otsiriza azatsanulira Mzimu Wake pa anthu onse. Anthu olimbikira ogwirizana akuyenera kuperekedwa ku uvangeli ndicholinga chokafikira zokolola zochulukira. Chitsanzo cha ntchito za atumwi mu Chipangano Chatsopano chinafunika anthu odzipereka kugwira ntchito kufikira ku cholinga chimodzi cha uvangeli.

Mukumbukire mmene Yohane ndi m'bale wake anali kusoka makoka pomwe Yesu anawayitana? Amayetsera kukonza chinthu chomwe chinali chakutha. Yesu anawayitana kuti atsiye makoka awo okutha ndikusinthanitsa kuti akhale asodzi a anthu. Pakuyankha, anakhal

mbali ya mgwirizano watsopano wa uvangeli. Pano funso nalo: kodi mutsalabe m'mbuyo kuyetsera kusoka makoka akale a kusiyana pakati pa ziphunzitso kapena mingingo, kapena mumva kuyitana kwa Khristu? Kodi mutsiya kalumikizanitsidwe kakale kopikitsana chifukwa cha kulumikizana kwatsopano kugwirizana ndicholinga chofikira dziko lapansi ndi Uthenga Wabwino?

## MAYESO OZIYESA NOKHA

1. Lembani mavesi otsogorera

---

---

---

---

2. Tanthauzirani “kulumikizana.”

---

---

3. Fotokozani mmene mpingo umalumikizanirana

---

---

4. Fotokozani Mphamvu za kulumikizana

---

---

5. Fotokozani kufunika kwa mphatso za uzimu ndi kulumikizana

---

---

6. Fotokozani mgwirizano omwe umadza chifukwa cha kulumikizana

---

---

7. Fotokozanin mmene kulumikizana kumagwirira ntchito

---

---

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

## ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Yesu anali ndikulumikizana polalikira uthenga. Anagwiritsa ntchito ophunzira nkhumu ndi awiri ndipo kanako anasakhaso ena 72 ndipo anawatumiza kunja, awiri awiri, mizinda ndi madala onse omwe Iye amkayenera kupitako (Luka 10:1). Pamene ophunzira wina anapeza wina amene sanali nawo mu” gulu” lawo akutumikira machiritso ndi mamasuridwe, anakamufusa Yesu ngati akuyenera kuletsedwa. Yesu anawonetsera “kulumizikana” poyakha. Werengani zokhudza izi pa Marko 9:38-40.
2. Utumiki wa Paulo unayamba chifukwa chazotsatira cha kulumikizana. Mzimu Woyera anayakhula ku mpingo waku Antioki ndipo Anati, “Mundipaturire Ine Barnaba ndi Saulo ku ntchito imene ndinawaitanirako.” Sanayitane munthu mmodzi koma gulu (Machitidwe 13:1-3). Paulo ndi Banaba anali oyambirira mukulumikizana kumeneku. Ena amene anazalumikizidwa kukhala mbali imodzi ya utumiki wa Paulo chifukwa cha uvangeli ndi awa:

- Yohane Marko	Machitidwe 13:5
- Sila	Machitidwe 15:22
- Timoteo	Machitidwe 16:1
- Luka	Machitidwe 16:10
- Priskila ndi Akula	Machitidwe 18;18
- Erasto	Machitidwe 19:22
- Sopatro	Machitidwe 20:4
- Aristarko ndi Sekundo	Machitidwe 20:4
- Gayo	Machitidwe 20:4
- Trofimo	Machitidwe 21:27-29
- Tukiko	Aefeso 6:21
- Tito	Agalatiya 2:1
- Dema	2 Timoteo 4:10
- Epafrodito	Afilipi 2:25
- Tertio	Aroma 16:22

3. Popeza kulumikizana kapena utumiki wa nthupi wawoneretsedwa bwino mmalemba, nde nchifukwa chiyani anthu amaukana? Zotsatirazi ndi zifukwa zodziwika bwino zomwe anathu samagwirizanirana. Zimenezi zikuyenera kugonjetsedwa ngatri tikufuna kuti tipambane polumikizana ndi ena.

- Timawopa kuluza ulamuliro: Nthawi zambiri timayamba kuganiza kuti tiluza ulamuliro wanthu pa bungwe kapena pampingo kwa ena.
- Timaika chidwi pazosephana zanthu mmalo mwapa zolinga zofanana ndi udindo: Timakhazizika pazomwe tikusephana ndi ena malo pazomwe tikufanana nawo kuti ndife amodzi mwa Khristu ndipo cholinga chanthu tonse ndi uvangeli.

- Timawopa kuluza thandizo: Timakhala ndi matha kuti ngati titagwirizane ndi ena, chithandizo chomwe timafuna chautumiki chizipita kwa iwo malo kwa ife.
- Timawopa kuluza anthu: Atsogoleri nthawi zina amakhala ndi mantha kuti anthu otsatira mpingo wawo angawasiye mkukalowa gulu kapena mpingo wa enawo.
- Timawopa kunyalanyaza: Chifukwa chakuti tiri ndi kusiyana pang'ono paziphunzitso, timawopa kuti tinyalanyaza ngati titayanjane ndi ena. Sitikuyenera kunyanyaza pa zinthu zachikhalidwe zanthu ndi ziphunzitso zonama, koma kusiyana kuchepa pachiphunzitso zisaloledwe kutchinga kulumikizana pa uvangeli.
- Chikhalidwe chanthu chauchimo chimapangitsa kuti tizikhala patokha: Ichi nchifukwa chake kuyesedwa kwa Eva kunatheka. Amkafuna kuti akhale payekha osadaliranso Mulungu. Kukhala pa wekha ndichikhalidwe chosakhala chaumulungu.



## CHIYAMBI CHA GAWO LACHIWIRI

### “PAMENE MUKUPITA” ...

Muthenga wabwino mu Chipangano Chatsopano, Yesu sanatume wina aliyense kukalalikirira Uthenga Wabwino popanda kuwalamula iwo kuti akachilkitse ndikumasa. Anawauza iwo “Pamene mukumuka... kachilitseni odwala, katulutseni ziwanda...”

Pamene khamu linabwera kuzachitsidwa ndi kuzamasulidwa, kholola la uzimu lianayamba kuchuluka mwasanga mokuti antchito ambiri atsopano anayamba kufunika. Sipanakhalitse pamene ophunzira makumi asanu ndi awiri anapezeka ndipo anatumizidwaso kuti akalalikire, akaphunzitse, ndikutiso akamasule.

Kunali kuwonetsera kwa mphamvu kumeneku pamene anamuka komwe kuanachititsa kuti Uthenga Wabwino ufalikire mwachangu kudziko lonse. Pachifukwa chimenechi, mbali iyi ya **“Kutumphukwa uvangeli”** ikukhazikika kwambiri pautumiki wa kuchilitsa ndi kumasa komwe kumatsatana ndi kulalikirira ndi kuphunzitsa Uthenga Wabwino.

Chaputala 16 chikupereka chiyambi cha utumiki wochilitsa ndi mamasulidwe. Chaputala 17 chikukamba za machitachita omwe amakhudza machilitso. Chaputala 18 chikukhazikika pa utumiki wa machiritso ndipo chaputala 19 chikukhudza kwambiri pa zautumiki wamamasulidwe.

## CHAPUTALA 16

### CHIYAMBI CHAMACHILITSO NDI MAMASULIDWE

ZOLINGA:

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba vesi yotsogolera.
- Kufotokoza mwamaganizidwe ena amene alipo pokhudzana ndimachilitso.
- Kuwonetsera magawo asanu amadwale.
- Kufotokoza “Machilitso akumwamba”.
- Kuloza komwe matenda amachokera.
- Kufotokoza zifukwa zodwalira.
- Kufotokoza mathero awiri amatenda.
- Kukambirana zolinga zamachilitso ochokera kumwamba.

VESI YOTSOGOLERA:

**Kuti kumwamba ndi dziko lapansi zicoke nkwapafupi, koma kuti kalemba kakang'ono ka cilamulo kagwe nkwapatali.**

**Yense wakusudzula mkazi wace, nakwatira wina, acita cigololo; ndipo iye amene akwatira wosudzulidwayo, acita cigololo. (Luka 16:17-18)**

### CHIYAMBI

Chaputalachi chikukamba za utumiki wanachiritso ndi mamasulidwe omwe okuyenera kulalikiidwa ndikuwonetseredwa monga ngati gawo limodzi la Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu. Mau oti “machiritso ndi mamasulidwe agwiritsidwa ntchito mosithanasithana muphunziro lino. Onse akukamba za umphumphu wa nthupi, Moyo, ndi mzimu zomwe zakambidwa malemba.

Mu mphunziro lino muphunzira magaganizidwe amene alipo pokhudzana ndi machiritso ndi mamasulidwe ndi kuphunzira kufunikira kwa kukuphunira kwa phunziro lino. Muphunziraso chiyambi ndi chifukwa cha matenda, mphatso yamachiritso, ndi zolinga za machiritso.

### MAGANIZO AMENE ALIPO OKHUDZANA NDI MACHILITSO

Choyambirira, nchoyenera kuzindikira magaganizo amene alipo omwe mukumane nawo pamene mwayamba kutumikira mu muutumiki umenewu. Pozokhudzana ndi machiritso ndi mamasulidwe, amabiri okhulupirira ambiri...

**ONYALANYAZA:**

Ena asamawabadila chifukwa chachenjezo lomwe Baibulo linapereka zokhudzana ndi zozizwa zachinyengo (Marko 13:22-23). Amatenga mawu awa ngati chenjezo pophudzana ndi zozizwa zonse. Ene amakhulupira kuti machilitso ndi khambakamwa chabe basi, ndipo amakana kuti machilitso atha kukhala kuwonerkerera ndimaso pochilitsa nthenda. Ena amawakayikira chifukwa cholephera kuyakha mafunso onse okhudzana ndi madwale ndi kuzuzika.

Ena samalabadira machilitso chifukwa chamatha kuti antha kulepphera. Zikuwoneka kuti pamakhala kaganizidwe kawiri. Tikamapepherera zachuma, nzeru ndi zina timapepherera molimbika ndi, chikhulupiriro, koma timakhala amatha tikamapepherera machilitso. Ena samazindikiraso mmene kaganizidwe ndi kukhala ndi mtima ongofuna zinthu mmene zawawongera. Ambiri “amakhulupirira akawona” ndipo oterewa amazidwa ndi zam’dziko osati zakumwamba.

#### **AMAKANA:**

Anthu ena amakana machilitso ndi mamasulidwe lero chifukwa alibe kulongosola kweni kweni komaso sanakumane nawo machilitso. Mu Uthenga Wabwino wa Chipangano Chatsopana chili ndi magawo makumi awiri asanu ndi limodzi omwe amawonetsera machilitso akuthupi. Buku la Machitidwe liri ndi magawo asanu. Machilitso akuthupi akambadziso pa 1 Akoritno 12:8-11 ndi 28-30. Yakobo 5:13-16 ikupereka malangizo amveka bwino amomwe tingapepherere odwala.

Palibe chilichonse chomwe makalata akusitha za chiphunzitsa cha Uthenga Wabwino pazamachilitso. Kupepherera odwala kunkatengedwa kukhala chinthu chachizolowezi panthawi imene makalata amkalembedwa, ndipo palibe chimene chimawonetsera kuti machiritso ochokera kumwamba anali odabwitsa mu mpingo oyamba.

#### **AMASOKONEZA:**

Anthu ambiri amasokoneza machilitso ndimamasulidwe ndi chikhalidwe cha munthu zomwe zili zosagwirizana ndi Mau a Mulungu. Muphunzira zina mwa zikhalidwe zimenezi mu chaputala chotsatila.

Ena amasokoneza ndizomwe akumana nazo chifukwa kale anapephererapo machilitso ndipo sanalandire. Koma tikuyenera kukhazikitsa chikhulupiriro chanthu pa Mau a Mulungu, osati pa zomwe takumana nazo (kapatula pokhapo pomwe zomwe takumana nazo zikugwirizana ndi Mau a Mulungu). Chitsanzo choipa cha machilitso chimasokoneza nkhani imeneyi chifukwa anthu ene amakhulupira miyambo, anthu amachilitsidwa ndi ndalama, chinyengo, ndiposo amakhazikika kwambiri poyang’ana machilitso akunthupi mmalo mwa machilitso amabali zonse.

Machilitso ndi mamasulidwe amasokonezedwaso chifukwa chosamvetsa bwino. Choonadi chilichonse, posatenga kuti ndichotani, chikakhazikika pochotsera choonadi china ndekuti choonadicho chimakhala ndizolakwika zina pamapeto. Mwachitsanzo, kukhazikika kwambiri pa udindo wamachilitso kwachititsa odwala ambiri kukhala ogonjetsedwa ngati iwo salandira pompo machilitso.

#### **KUCHEDWETSA:**

Anthu ena achedwetsa potumikira machilitso ndi mamasulidwe chifukwa alibe mayankho kuchina chilichonse. Samamvetsetsa chifukwa chani ena akuchilitsidwa pamene ena ayi. (Muphunzira zambiri za izi muchaputala chotsatira)

Mayankho ena amabwera pamene mwayamba kutumikira ndikukumana ndi mphmavu Ya machilitso a Mulungu. Mafunzo ena sazayakhidwa nkomwe. Ngati mungazindikire “zifukwa zonse” kukhudzana ndi zinthu zonse ndekuti simuzamufunaso Mulungu. Baibulo limati

“timangodziwa mdera mdera.” Machiritso okhudza madwale ndi mazunzo nthawi zonse azakhala odabwitsa chifukwa chozizwa chachoipa chikugwirabe ntchito (2 Atesalonika 2:7).

### **KUFUNIKA KWA KUPHUNZITSA KUYENERA**

Kusitha kaganizidwe komwe kulipo pano pokhudza machititso ndi mamasulidwe kukuwonetsera chifukwa chomwe kuli kofunika kwa kuphunzitsa koyenera pa phunziro limeri. Ambiri akuwonongeka kunthupi ndi kuuzimu chifukwa sazindikira zomwe Mau a Mulungu aluphunzitsa zokhudzana ndi machiritso.

#### **Anthu anga akuwonongeka chifukwa chakusadziwa. (Hoseya 4:6)**

Machilitso (onse) ndi mbali imodzi ya Uthenga Wabwino wa ufumu omwe unalamulidwa kuti ufalikire (Luka 16:15-18). Yesu anatitana kuti tikalalikire, tikaphunzitse, tikachilitse, ndikumasa. Machilitso ndi mamasulidwe sakuyenera kusiyidwa, koma akuyenera kutsindikizidwa posachotsapo posachotsapo ziwirizi.

Baibulo limawonetsera kuti mipimgo yanthu ikuyenera kukhala malo amachilitso (Luka 14:16-24). Tikuyenera kuwona anthu akuchilitsidwa osati akuthawa.

#### **Ndipo lambulani miseu yolunjika yoyendamo mapazi anu, kuti chotsimphinacho chisapatulidwe m'njira koma chichiritsidwe. (Ahebri 12:13)**

Monga ngati okhulupirira, ndi tchimo ngati sitikugawa Uthenga Wabwino wa machiritso ndi mamasulidwe kwa otayika ndi afuka kudzikira. Baibo likuti:

#### **Potero kwa iye amene adziwa kuchita bwino ndipo sachita, kwa iye kuli tchimo. (Yakobo 4:17)**

Mulungu wapereka chenjenzo lokhwima kwa atsogoleri amene amakana machiritso:

**Zofoka simunazilimbitsa; yodwala simunaiciritsa, yotyoka simunailukira chika, yopitikitsidwa simunaibweza, yotayika simunaifuna; koma munazilamulira mwamphamvu ndi moopsa...**

**Ndidzafuna yotayika, ndi kubweza yopitikitsidwa, ndi kulukira chika yotyoka mwendo, ndi kulimbitsa yodwalayo; koma yanenepa ndi yolimba ndidzaziononga, ndidzazidyetsa ndi ciweruzo... (Ezekieli 34:4,16)**

### **KUYAMBA NDI MAGANIZO ABWINO**

Pamene mukuyaphunzira phunziro la machiritso ndimamasulkidwe, mukuyenera kuchita choncho ndi kakaganizidwe kabwino. Mukuyenera kusiyana zomwe munakuna nazo kale ndi miyambo yomwe munauzidwa. Mukuyenera kukhala ophunzitsika. Chimodzi mwa zizindikiro za nzeru yochokera kumwamba ndichakuti imakhala yovomera maganizo ena (Yakobo 3:17). Ngati mukhala wosaphunzitsika ndekuti mu uzimu mukhala pachipsyeyo.

Kumbukirani kuti tchimo loganizira ndikuyika Mulungu mkaganizidwe kanu kochepe. Anzake a Yobu anachimwa poganiza munjira imeneyi. Padziko lapansi kugwiritsa ntchito pa zomwe munthu wakumana nazo mkolakwika. Yambani phunziro ili ngati simunavepo ziphunzitso zachikhalidwe chamunthu pa zimenezi. Landirani chomwe Mau a Mulungu akunena: Ngati akuti mwachiritsidwa, akhulupirireni. Ngati akuti tisanjike manja pa odwala, chitani choncho. Chomwe akuti Mulungu achita, yembekezerani kuti achitadi.

Musasakesake njira yolandilira kapene yotumikirira machiritso. Baibulo silipereka njira, ngakhala ndondomeko zochuluka zimaonetsedwera ndipo tizikambirana zonse. Mmallo mofunafuna njira, ingozindikira kuti Wochiritsa alimwainu. Sakanisakani njira yokulitsira kuzindikira kwanu ndi ubwezi weni weni ndi Wochiritsayo.

Yesu ndi Mzimu Woyera amakhala mwainu. Machiritso samasakidwa kunja, koma mumaphunzira kuwatulitsa kuchokera mkati. Mufunefune kumvetsa bwino ndondomeko zomwe zimatulutsa mphamvu yomwe iri mkati.

Zindikirani kuti ngati mukutsatadi chitsanzo cha utumiki wa Yesu wa machiritso ndeukti inu mu:

1. Muzakhala kapolo osati “mbuye”: Marko 10:44
2. Kulema, osati kulemera: Marko 6:31; Yohane 4:6; Machitidwe 3:6
3. Kukumana ndikusakhulupirira kwa anthu ena: Marko 13:58
4. Kukumana ndi chizuzo chochokera kwa atsogoleri achipembedzo: (Ena mwa iwo alingati Afalisi... amene amakhala okhudzika kwambiri ndi chilamulo ndi makhalidwe amoyo): Luka 6:6-9
5. Kukumana ndi chizuzo chochokera kwa amene akuyandikirani: Marko 6:4 ndi Mateyu 13:58
6. Kupewa kulengeza malo moyisaka: Marko 8:36; Mateyu 8:4
7. Kukana kufuna kupindula inu eni kapena kupeza zinthu kupyolera mu mphamvu ya Mulungu: Machitidwe 8: 18-24
8. Kukana kupatsidwa ulemu: Machitidwe 14:8-18

## MACHIRITSO AKUMWAMBA

Pali mitundu yambiri yamachiritso padziko lero:

**-Machiritso ochiza maganizo:** Awa ndi mau amagwiritsidwa ntchito pokamba za malingaliro pazinthu, ufiti, zamatsenga, ndi machiritso a asing'anga.

**-Machiritso auzimu:** kuli komwe machiritso auzimu amachokera komwe sikuli kwa Mulungu, nde sitigwiritsa ntchito mau amenewa mu phunziro lathu. Satana naye antha kuwonetsera ntchito za uzimu (Eksodo 7:8-13).

**-Machiritso amakhwala:** mtundu wamachiritso umenewu umaperekedwa ndi a dokotala, anamwino, zipatala, ndi makhwala, monga mmene titaphunzirire tiwona kuti machiritso obwera ndi makhwala sakutsutsana ndi Mau a Mulungu, koma akukuza kukoma mtima Kwake.

**-Machiritso akunthupi:** Machiritso amene amachitika kupyolera kunthupi amakhala kuti wawachita ndi Mulungu. Machiritso akunthupi amawonetsera Umulungu Wake ndi ntchito yayikulu imene akuichita muthupi la munthu. Machiritso akunthupi

amaphatikizaponso kugwiritsa njira zina zachilengedwe monga ngati kudya zakudya zamagulu, mavitamini, kupumula ndizina zotero.

**-Kuchiritsidwa mwachikhulupiro:** Mau awa kawirikawiri amagwiritsidwa ntchito pofunakuwonetsera kuti machiritso amabweretsa ndi Mulungu. Sitigwiritsa ntchito mau amenewa, chifukwa kumapeto kwake amakhazizika poyang'anitsitsa chikhulupiro cha yemwe akutumikirayo kapenaso amene akulandira kutumikiridwako.

**-Machiritso akumwamba:** Mau oti “kumwamba” amaiki chidwi chonse pa Mulungu, osati kuyakha kwachikhulupiro kwa munthu. Mtundu wamachiritso umenewu ndiosiya ndi mitundu ina ija.

Muphunziro lino tigwiritsa ntchito liwu loti machiritso akumwamba. “Kumwamba” kumalozera kwa Mulungu mmodzi wowona, ndi chikhalidwe Chake, monga mmene zawonetseredwa Mau Ake, Baibulo loyera. “Machiritso” amatanthauza kuti kuchiza kapena kupangaso kukhala bwino. Machiritso antha kukhala kupulutsidwa kuzauzimu, zakunthupi, machitachita, kaganizidwe ndi kuzuzidwa ndi ziwanda. Machiritso sinjira yozembera matenda. Matupi anthu ali “munjira yopita kovunda” ndiposo ndi otsekuka kuchiwembu cha satana ngati tikukhalabe mu dziko muno. Machiritso akumwamba ndipomwe Mulungu mmodzi wowona awonetsera chikhalidwe Chake, akwaniritsa malonjezano Ake, ndikuchitapo kathu pakulowa mmalo kwa Khristu pochiza munthu ndikumpanga iye kukhala wagwiro mu nthupi lake, moyo (Maganizo, chifuniro, ndimaivaimva) ndi mzimu.

Machiritso akumwamba atha kukhala apompopompo (Mozizwitsa) kapenaso apang'onopang'ono (mopitirira). Ngakhale machiritso amozizwitsa, apompopompo amawonetsewka kupezeka kwakumwamba ndi mphamvu ya Mulungu, machiritso akumwamba amene amachitika mwandondomeko siochepera kumachiritso kusiyana ndi omwe amachitika mwapompopompo. (Onani Marko 8:22-25)

## **MADWALE NDI MATENDA**

Pamene tikuyakhula za kudwala kapena matenda timatanthauza chikhalidwe chomwe chiri chosagwirizana ndi ndi mmene ziriri kunmwamba mmene Mulungu analengera. Pali magulu asanu amatenda:

### **KUDWALA KWA UZIMU:**

Kudwala kwa uzimu ndi tchimo. Ngati sithana nalo, ndi dula moyo wauzimu. Machiritso a thenda ya uzimu ndi kukhululukidwa kwa tchimo kupyolera mwa Yesu Khristu. Ndi machiritso opambana kuposa onse, monga ngati kuti ukadaulo wamakhwala ndi machiritso auzimu sangathe kuchita kanthu pamadwale awa.

### **KUDWALA KWAKUTHUPI:**

Kudwala kukhoza kubwera chifukwa chakusokonekera kwa thupi. Ndi mavuto oti akhoza kuzindikiridwa ndikuwonedwa ndi akatswiri achipatala. Kudwala kwa thupi kutha

kubweranso chifukwa chakusokonera kapena kusagwira bwino kwa ziwalo zathupi. Awa ndi matenda amene amabwera chifukwa chakusokonekera kwa chiwalo chimodzi zomwe zimapangitsa kuti thupi lonse lisokonekere. Matenda odziwika bwino ndi monga matenda a mtima, kuthamanga kwa magazi, shuga, tizilonda tammimba ndi ena otero. Ngati matenda akhalitsa osachizidwa amatha kuwononga ziwalo zina. Chifukwa chakugwirizana kwa thupi la munthu, kudwala kwa mbali imodzi kukhoza kunkhudza nthupi lonse.

### **KUBWALA KWA MAIMVAIMVA:**

Kudwala kwa maimvaimva kumabwera chifukwa chamaimvaimva oipa monga ngati mkwiyo, kuwawidwa mtima, ndi zina zotero. Kuti izi zichiritsidwe Mulungu akuyenera kukhudza maimvaimva amkati. Ena amawatchula kuti “machiritso amkati,” ngakhale mauwa nthawi zina amagwiritsidwa ntchito molakwika ndipo amakuzidwa mkumatanthauza zomwe Baibulo silimaphunzitsa.

### **KUDWALA MISALA:**

Matenda amasila amayamba chifukwa chakudwalitsa nthawi yayitali, kukhumudwa, zilema zobadwa nazo ndi zina zomwe sizimabwera ndi satana.

### **ZIWANDA:**

Mwamatenda ena amene amabwera chifukwa cha ziwanda ndi monga kugwidwa ndi mizimu yoyipa, kuponderezedwa, komaso ziwanda zina zimachititsa munthu kudwala matenda amasila ndi matenda ena akuthupi. Matenda obwera ndiziwandawa amafuna machiritso ake apaderadera omwe amatchulidwa kuti mamasulidwe. Mamasulidwe ndi machiritso ndi ofanana, koma malemba amawasiyanitsa:

**Ndipo Iye anaitana pamodzi khumi ndi awiriwo nawapatsa mphamvu ndi ulamuliro pa ziwanda zonse, ndi zakuchiritsa nthenda.**

**Ndipo anawatuma kukalalikira Ufumu wa Mulungu ndi kuchiritsa anthu odwala. (Luka 9:1-2)**

### **KOCHOKERA MATENDA**

Kuli kumodzi komwe matenda amachokera, ngakhale pali zifukwa zambiri zomwe munthu angadwalire. Paulo anatsimikiza izi pamene anati “Pakutero ambiri adwala” (1 Akorinto 11:30). Satana ndemagwero azoipa zonse za padziko. Matenda ndi imfa zinalowa mdziko kupyolera pakuchimwa kwa munthu. (Werengani Genesis 1-3 ndi Yakobo 1:17). Satana kwake ndi kupha, kuba ndi kuwononga. Yesu nde magwero amaoyo ochuluka.

**Siikudza mbala, koma kuti ikabe, ndi kupha, ndi kuononga, Ndadza Ine kuti akhale ndi moyo, ndi kukhala nao wocuruka. Yesu anati iye anabwera kudzapulumutsa anthu osati kudzawaononga. Kuombola kumaphatikiza machiritso komanso kupulumutsa. (Yohane 10:10)**

Matenda ndi madwale ndi mbali imodzi yamatembelero, koma aGalatiya 3:13 akuti, “Mkristu anatiombola ife kuthembelero lachilamulo.” Thupi ndilake la ambuye. Silathu la ife tokha, matenda kapena madwale. Matenda amaononga thupi monga tchimo liononga mzimu. Nthenda imaba thanzi, chimwemwe, ndalama, nthawi, kuthekera, malingaliro, komanso

mphamvu. Imapha komanso kuononga. Ngakhaleso ngozi imaonanga. Ndendichachiziwikire kuti muzonsezi kuti “adani ena anachiti zimenezi” (Mateyu 13:12).

Chifukwa chakuti matenda ali ndi mizu yake mwa satana, mukuyenera kuikana monga momwe makanira mayesero ndi manchimo. Pamene mukukana mayensero ndi tchimo makhala kuti mukumenya khondo ya uzimu. pamene mukukaniza matenda makhalanso mukumenya khondo ya uzimu.

Satana amapereka chionongeko kudzera mumatenda. Ngakhale kut nthenda iliyonse siyochokera kumizimu yaziwanda, matenda amapezeka m’dziko chifukwa cha satana.

Nthenda iliyonse imachokera kutizilombo mmoyo. Monga mzimu apereka moyo ku thupi, satana naye apereka moyo kutizilombo. Monga mchilengedwe chadziko, Mulungu anatenga chamoyo nachichulukitsa kuti chikabweretse moyo.

Satana amasinthanitsa chabwino ndi choipa. Amabweretsa tizilombo, matenda nawachulutsa kuti akabweretse imfa.

Pamene mzimu woipa watulutsidwa, nthenda imafa thupi mwanu. pokhapokha ngati tizilombo tamoyo tilipo mthupi, nthenda imakhalanso ndikupitilizabe ntchito yake yoononga. Chifukwa chiyambi chamatenda chimachokera kwa satana, mphamvu zake zikuyenera kumangidwa kuzitulutsa kunja.

Ngati mumvetsetsa mmene Mulungu amaonera nthenda simudzakhala ndichikayiko komwe ichokera

-Mulungu amayitcha nthenda ukapolo (Yobu 42:10). Yesu anabwera kudzalalikira mamasulidwe ku ukapolo (Luka 4:18).

-Yesu amayitcha nthenda kumangidwa (Luka 13:16). Anabwera kudzamasula amsinga ndi choonadi (Yohane 8:32).

-Yesu amaona nthenda ngati kuponderezedwa ndipo anachiritsa iwo akuponderezedwa (machitidwe 10:38).

-Baibulo nthenda ndi imfa ndi adani (1 akorinto 15:26).

-Nthenda imaonedwa ngati zonyansa (masalimo 41:8).

## **ZIFUKWA MADWALE**

Pali njira imodzi yomwe imabweretsa madwale, kaya kuthupi kapena ku uzimu, koma satana ndiye amabweretsa nthendazi. Koma zifukwa zomwe nthenda zimabwera pa ife ndi zosiyana siyana:

### **KUYANG’ANILA MZIMU WACHILAMULO:**

Pamene munthu anachimwa, imfa inayamba kugwira ntchito yachinyengo mthupi:

**Chifukwa chakenso, pamene munthu wachimwa nalowa m’dziko, imfa ndi tchimo; ndipo imfa inadutsa pamunthu aliyense, pakuti onse anachimwa. (Aroma 5:13).**

**Pakuti mphoto yake ya uchimo ndi imfa. (Aroma 6:23)**





zomwe amapangira ziwembu. Ngakhale achita chiwembu kuthupi chomwechonso ku uzimu, alibenso ufulu okhala mmoyo wanu wakuthupi koma kukhala kumoyo wanu wa uzimu.

Machitidwe amphamvu asatana kuthupi la okhulupilira akhoza kulinganizidwa ndi nkondo ya gerila. Ndipo alibe ufulu weniweni mmadera monse koma amafuna kumangochita mulimonse.

### **CHIONONGEKO CHA THUPI KUTI MZIMU UPULUMUTSIDWE**

Mulungu amalolera anthu ena kwa satana kuti akaonongedwe ndicholinga choti akalandire mwambo. Mulungu samapereka matenda pa iwo, koma amalolera kuti zichitike ndithu. Mukhoza kuwerenga pa 1 Akorinto 5:1-7.

“Muchionongeko cha thupi, “mpingo umamutembenuza munthu ochimwa kwa satana kuti akaonongeke ku thupi ndikuti mzimu ukapulumsidwe. Baibulo likunena:

#### ***Kodi zingachitike bwanji:***

1. Mu umodzi.
2. Mu uzimu ndi mphamvu ya ambuye.
3. Mudzina la ambuye.

#### ***Nchifukwa chani zimachitidwa:***

1. chiwerewere.
2. khalidwe loipa kuposa ladziko.
3. kudzikuza.
4. Kusowekera kulapa.
5. uchimo pakati pa anthu aMulungu.

#### **Cholinga chake:**

1. Munthu: chionongeko chathupi ndicholinga kuti mzimu ukapulumsidwe.
2. Machitidwe: Kuchotsa choipa mwachangu chisanaononge ena.

### **KUPHWANYA MALAMULO A CHILENGEDWE CHA MULUNGU:**

Matenda ena amabwera pa ife anthu chifukwa tinaphwanya malamulo achilengedwe cha Mulungu. Mwachitsanzo:

-Kudya kosayenera.

-Kugwira nchito mopyola muyeso, kupanga zinthu mwaphuma.

-kupumula kosakwamira.

-kusadziletsa komwe kumabweretsa mkwiyo, kuwawidwa mtima ndi zina zotero.

-kusowekera ubale wabwino ndi anthu ena (kuwawidwa mtima, kusakhululuka).

-masewera olimbitsa thupi (kuchulutsa kapena kuchepetsa).

-kumwa mankhwala ozunguza bongo komanso kumwa mowa mwa uchidakwa. Kuyika zinthu za poyizoni mthupi.

-kumphwanya chilengedwe cha lamulo monga ngati lamulo loti chilichonse chokwera mmwamba chitsike pansu.

Mwadaladala kuzipezeketsa muchiopsezo kudzera mumachita chita angozi komanso kukana kugwiritsa ntchito zida zodzitetezera (monga kumanga lamba pampando wamugalimoto, kuvala magalasi pomwe munthu ukugwira ntchito, chipewa chozitetezera pomwe ukugwira ntchito ya zomangamanga).

### **KUSAZINDIKIRA KWENIKWENI THUPI LA CHRISTU:**

Paulo anati ambiri anali ofooka ndi odwala chifukwa sanazindikira bwino thupi la christu ndi kutenga mgonero osafunikira.

### **ZOTSATIRA ZA MATENDA**

Zotsatira zamatenda zikhoza kukhala.....

### **CHIFUKWA CHA ULEMELERO WA MULUNGU:**

Munthu akachiritsidwa Mulungu amalandira ulemelero kudzera mu maumboni, moyo, ndi mu utumiki. Yesu ananena za munthu osaona;

**...Sanachimwa ameneyo, kapena makolo ake, koma kuti nchito za Mulungu zikaonetsedwe mwa iye. (Yohane 9:3)**

Ulemelero wa Mulungu umapita komwe kuli machiritso apamwamba, inde, koma ulemelero ukuyeneranso kupita kwa Mulungu chifukwa cha machiritso omwe thupi limapanga lokha. Mulungu analenga thupi ndipo anaonetsera chilengedwe ndi mphamvu yake yamachita chita nthupi.

ulemelero ukuyenera kupitanso kwa Mulungu chifukwa cha machiritso obwera chifukwa chothandizidwa kuchipatala. Baibulo limati mpatso iliyonse ya bwino imachokera kwa Mulungu, ndimonga mankhwala, timichere tofunika mthupi ndi zinthu zina zomwe zili zotithandiza ife kuthupi. Mankhwala ambiri amapangidwa kuchokera zinthu za chilengedwe monga zomera ndi zinthu zina zomwe Mulungu anazilenga munthawi yoyambirira.

**...sanadziwa kutindinawachiritsa iwo (Hosea 11:3)**

Nthawi zina machiritso amachedwa ndikuti munthu akhoza kudzachiritsidwa pambuyo pake kapena pang'onopang'ono. Zitsanzo:

-Zakaria sanachiritsidwe mpaka kubadwa kwa Yohane: Luka 1:20

-Hanna sanabereke mwana kufikira nthawi yoyikika ya Mulungu: 1 Sammueli 1:5-19

- Abraham ndi sara sanabereka mwana kupatula kuti Abrahamu anali wachikhulupiliro, kufikira nthawi yoyikika ya Mulungu;(Aheberi 11:11)

### **MATENDA OKUTENGERA KU IMFA:**

Ku Yohane 11:4 Yesu anati nthenda ya Lazaro sinali yomutengera ku imfa. Zomwe zikuthanthauza kut pali nthenda zokutengera ku imfa. Pali mitundu iwiri ya imfa yomwe baibulo limafotokoza. Ena omwe amene aperekedwa kuchiwonongeko cha chanthupi amamwalalira mwansanga ndicholinga chakuti mzimu wawo ukhoza kukapulumuka.

Munthu aliyense ali ndi nthawi yoyikika yoti amfe (Mlaliki 3:2; Ahebri 9:2). Ngakale Elisa, mneneri wamphamvu wa Mulungu anachita zozizwa zambiri zamachiritso, anadwala “nthenda ija adafa nayo” (2 Mafumu 13:14). Ndizotheka kungoleka kupuma osadwala.

**Mukalanda mpweya wao, zikufa, nizibwerera kupfumbi kwao. (Salimo 104:29b)**

Kwa okhulupirira, zotsatira zaukamba zikhoza kukhala mbali zonse. Mose monga ngati munthu wokalamaba analibe zovuta za kukula kwake. Yoswa anali “wokalamba”. Mulungu amasunga ena mwauzimu, pamene ena akukumana ndi zovuta chifukwa cha ukamba. Mulungu amatisunga kaya matupi anthu akutsata njira yachilengedwe yokalambira ndi kumwalira ndi matenda kapena akutetezedwa ndi mphamvu ya kumwamba. Cholinga chamachilitso sikuti mkusamwalira. Machiritso akumwamba safikira zomwe zirizonse zimene makhwala amachita. Ngakhale onse amene anaukitsidwa ndi Yesu kwa akufa mapeto ake anazafanso.

Pamene okhulupilira wamwalira, ndimachiritso amphumphu kumoyo osatha. Timalakwitsa pakukhala ndimoyo wozipatsa malire ndi nthawi mmalo mokhala mmoyo osatha. Ngati okhulupilira, tikukhala mmoyo wosatha ngakhale pomwe tili amoyo mmoyo uno ingakhalenso pomwe tamwalira.

**MPHATSO ZA MACHIRITSO**

Mphatso za mzimu woyera zinapatsidwa kuthupi kuti zikamangilire kuthupi. Ndizo mphatso zamachiritso ndizopezekeratu kwa aliyense ndi kuchiritisa aliyense. Munthu sangagwiritse ntchito mphatso za machiritso pa iye yekha. Mphatsozi zimagwiritsidwa ntchito ndi mzimu woyera kudzera mwa munthu. Baibulo limati tikuyenera kufuna mphatso zomwe zili za bwino kwambiri:

**Koma funitsitsani mphatso zoposa. (1 Akorinto 12:31)**

Ukamapempherera za mphatso za mzimu wamachiritso, umakahalaso ukumuza Mulungu kuti akutkule kuchoka pomwe iwe uli kale. Monga okhulupilira onse alindi kuthekera ndi ulamuliro wakusanjika manja odwala kut achiritsidwe. Yesu anawonjezera zomwe iye anapatsidwa (Luka 5:22) timoteo anauzidwa kuti angokuza mphatso zomwe zinali mwa iye kale. (2tomoteo 1:3).

Pali mitundu yosinasiyana ya mphatso zamachiritso. Kuli mitundu yosiyana siyana ya matenda ndi mphatso zosiyana zamachiritso kuti akachiritse matendawo. Ngati Mulungu akufuna kuchiritisa kudzera munjira imodzi, sanakagwiritsaso njira zina zambiri zomwe zananedwa m’Baibulo.

Lingalilani njira zambiri zomwe Mulungu amagwiritsira ntchito pofuna kupulumutsa munthu. Kodi sangagwiritseso njira zambiri kuti abwretse machiritso? Njira kapena mphatso mwazokha sizimachiritisa kuposa kupulumutsa. Ndi njira zimene mphamvu ya Mulungu zimawonetsedwera. Mu Baibulo timapeza kuti machiritso anachitika po:

1. Kusanjika manja: Mtumiki kukhudza odwala.
2. Anthu kumukhudza mtumiki.
3. Kuyakhula mau kuchokera patali.
4. Kuyakhula mau pamaso pa odwala.
5. Kuchita naye wodwala maso ndi maso.

6. Kuchiritsa chifukwa chamapembedzero a anthu ena.
7. Kupemphera.
8. Ntchito ya chikhulupiriro: machiritso amene amachitika kudzera mu mphamvu ya chikhulupiriro chomwe wodwala alinacho.
9. Mitundu yosiyanasiyana yachikhulupiriro yomwe ikugwira ntchito.
  - a. Chikhulupiriro cha yemwe akutumikira.
  - b. Chikhulupiriro cha munthu yemwe akufuna machiritso.
  - c. Chikhulupiriro cha abwenzu.
  - d. Chikhulupiriro cha abale.
10. Anagwiritso ntchito zinthu zosiyanasiyana. Panalibe choyera mwachokha, koma zinagwira ntchito kukhala pamalo okumanira.
  - a. Mate.
  - b. Thope.
  - c. Nsalu zopemphereredwa.
  - d. Masamba a mkuyu.
  - e. Mphonje ya chovala cha mtumiki.
  - f. Chithuzithuzi cha mtumiki.
  - g. Mafuta.
  - h. Zaka makutu.
  - i. Madzi.
  - j. Kukhudza.
11. Zozizwa zapaderadera.

Mulungu amadzodza anthu ena ndi chikhulupiriro chamachiritso mwapaderadera (Monga mtumwi Paulo). Mwachitsanzo, Mulungu amagwiritisa ntchito anthu ena kuti atumikire mwapaderadera kwa amene akudwala khansa, ndi ena otero. Izi sizikutanthauza kuti tisatumikire madera onse ofunikira machiritso, chifukwa tinalamulidwa kuti tikachiritse odwala onse.

Okhulupirira onse anatumizidwa kuti akachiritse odwala, ngaakhale Mulungu nthawi zina amayenda mwapaderadera ndi mphatso zapaderadera, onse akuyenera kutenga mbali muutumiki wamachiritso. Nawo anthu amene Baibulo limanena kuti atenge mbali pamachiritso:

- Abusa (atsogoleri auzimu): Ezekeleli 34
- Akulu ampingo: Yakobo 5:14
- Okhulupirira wamba: Yakobo 5:16; Luka 16:15-18
- Onse amene ali ndi mphatso zapaderadera zamachiritso: 1 Akorinto 12:9
- Mpingo onse ndi malo amachiritso: Luka 14:16-24

### **CHOLINGA CHA MACHIRITSO**

Cholinga chodziwikiratu chamachiritso ndikumupanga wodwala kuti akhale bwino. Koma machiritso ndi mamasulidwe ali ndicholinga choposa kungopanga anthu kuti akhale bwino. Machiritso ndi mamasulidwe ndi:

## **KUWONETSERA CHIKHALIDWE CHA MULUNGU:**

**Yehova ndiye wacisomo, ndi wacifundo; Osakwiya msanga, ndi wa cifundo cacikuru.**

**Yehova acitira cokoma onse; Ndi nsoni zokoma zace zigwera nchito zace zonse. (Masalmo 145:8-9)**

**Ndipo Yesu anagwidwa cifundo, natansa dzanja namkhudza iye, nanena naye, Ndifuna; khala wokonzedwa. (Marko 1:41)**

## **KUMUKWEZA MULUNGU:**

**Ndipo makamu ambiri a anthu anadza kwa Iye, ali nao opunduka miyendo, akhungu, osalankhula, opunduka ziwalo, ndi ena ambiri, nawakhazika pansa pa mapazi ace:**

**Ndipo Iye anawaciritsa; kotero kuti khamulo linazizwa, pakupenya osalankhula nalankhula, opunduka ziwalo nacira, ndi opunduka miyendo nayenda, ndi akhungu napenya, ndipo iwo analemekeza Mulungu wa Israyeli. Mbali yomukweza Mulungu imakhudzanso kumuopa Mulungu. Machiritso amabweretsa zimenezi: (Mateyu 15:30-31)**

**Koma m'mene anawaopsanso anawamasula, osapeza kanthu kakuwalanga, cifukwa ca anthu; pakuti onse analemekeza Mulungu cifukwa ca comwe cidacitika. (Macitidwe 4:21)**

Mbali yina yomukweza Mulungu imakhuza mantha apa Mulungu. Machilitso amatsatira izi:

**Koma panadza mantha pa anthu onse; ndipo 5 zozizwa ndi zizindikilo zambiri zinacitika ndi atumwi. (Macitidwe 2:43)**

## **KUTSIMIKIZA KUTI YESU NDI MPHULUMUTSI NDI WODZODZEDZA:**

Werengani Mateyu 8:14-17 mu Baibulo mwanu. Machiritso amene alembedwa apa akutsimikiza mau a mneneri:

**...Iye yekha anatenga zofoka zanthu, nanyamula nthenda zathu. (Mateyu 8:17)**

Mu Luka 5:18-26 kuchiritsidwa kwa olumala ndikukhululukidwa kwa machimo ake kunatsimikiza kuti Yesu ndi mpulumutsi komaso ngati mchiritso. Nawo umboni wina wamalemba omwe amatsimikiza kuti Yesu ndi mpulumutsi:

**Ngati sindicita nchito za Atate wanga, musakhulupirira Ine. Koma ngati ndicita, mungakhale simukhulupirira Ine, khulupirirani nchitozo; kuti mukadziwe ndi kuzindikira kuti Atate ali mwa Ine, ndi ine mwa Atate. (Yohane 10:37-38)**

**Ndipo zizindikilo zina zambiri Yesu anazicita pamaso pa akuphunzira ace, zimene sizinalembedwa m'buku ili; koma zalembedwa izi kuti mukakhulupirire kuti Yesu ndiye Kristu Mwana wa Mulungu, ndi kuti pakukhulupira mukhale nao moyo m'dzina lace. (Yohane 20:30-31)**

## **KUTSIMIKIZIRA NTHENGA NDI UTHENGA:**

**Ndipo mkazi anati kwa Eliya, Ndizindikira tsopano kuti ndinu munthu wa Mulungu, ndi kuti mau a Yehova ali m'kamwa mwanuwo ngoona. (1 Mafumu 17:24)**

**Cifukwa cace anakhala nthawi yaikuru nanenetsa zolimba mtima mwa Ambuye, amene anacitira umboni mau a cisomo cace, napatsa zizindikiro ndi zozizwa kuti zicitidwe ndi manja ao. (Macitidwe 14:3)**

**Koma pakuona kulimbika mtima kwa Petro ndi Yohane, ndipo pozindikira kuti ndiwo anthu osaphunzira ndi opulukira, anazizwa ndipo anawazindikira, kuti adakhala pamodzi ndi Yesu. (Macitidwe 4:13)**

## **KULIMBIKITSA KALANDIRIDWE KA UTHENGA WABWINO:**

**Amene ife tinalandira naye cisomo ndi utumwi, kuti amvere cikhulupiriro anthu a mitundu yonse cifukwa ca dzina lace. (Aroma 1:5)**

Ndikosavuta kuwauza anthu za Uthenga Wabwino pamene achiritsidwa. Pali zitsanzo zambiri za izi mu buku la Machitidwe. Machiritso amatsekula makomo a Uthenga Wabwino wa chipulumutso kuti ugawidwe, kudzadzidwa kwa Mzimu Woyera, ndikukula kwa mpingo. Onani Machitidwe 2:42-47 ndi 5:14 pa zitsanzo.

Ngakhale machiritso amalimbikitsa kuti Uthenga Wabwino ulandiridwe, nthawi zonse kumbukirani kuti samalowa mmalo mwakulalikira Uthenga Wabwino wachipulumutso. Mau akuyenera kulalikiidwa motsatana ndikuonetsera mphamvu kupyolera kuchiritsa ndikumasa ndicholinga chobweretsa anthu muubwere wabwino ndi Mulungu. Nthawi zonse kumbukirani kuti ndi mau amene amalenga chikhulupiriro chopulumutsa, kuchiritsa, ndi kumasulu.

Machiritso ndi chida champhamvu polalikira Uthenga. Muzolembedwa zokhudza machiritso m'malemba:

-Malo okwana nkhumu kasanu ndi kawiri, machiritso anachitika munthawi yomwe uthenga umkalalikiidwa:

Mateyu 4:24; 8:16; 9:2-8; 9:32-33

Marko 1:23-28; 9:14-27; 10:46-52

Luka 8:42-48; 13:10-13, 16; 14:1-4; 17:11-19

Yohane 4:28-30; 5:1-9, 14; 9:1-7

Machitidwe 3:1-10; 8:5-8; 14:8-10

-Malo okwana khumi asanu ndi limodzi, machiritso anali zotsatira za kulakira Uthenga Wabwino:

Mateyu 9:2-8; 9:32-33; 12:9-13

Marko 1:23-28; 5:1-13, 18-20; 7:32-37; 9:14-27

Luka5:12-14; 13:10-13, 16; 17:11-19

Yohane 4:28-30; 9:1-7

Mchitidwe 3:1-8; 8:5-8; 9:32-35; 14:8-10

-Mumalo makumi awiri ndi limodzi mwa malo makumi awiri asanu ndi limodzi, kunali kulalikira Uthenga kapena zotsatira.

### **KUKHAZIKITSA UFUMU WA MULUNGU:**

**Ndipo ciritsani odwala ali mamwemonimunene nao, Ufumu wa Mulungu wayandikira kwa inu. Koma ku mudzi uli wonse mukalowako. (Luka 10:9)**

**Ndipo Yesu anayendayenda m'Galileya monse, analikuphunzitsa m'amasunagoge mwao, nalalikira uthenga wabwino wa Ufumu, naciritsa nthenda zonse ndi kudwala konse mwa anthu. (Mateyu 4:23)**

Pamene mukutumikira machiritso, kumbukirani kuti ufumu sunakhazikitsidwe mwanthunthu. Ufumu ukazakhazikitsidwa mwanthunthu matenda ndi imfa sizizakhalaposo. Iziso zirichomodzimodzi ndi matenda. Kudwala ndi chilango chamachimo anthu akale. Tikhoza kuwomboledwa kumphamvu yake panakali pano, koma osati kupezeka kwake mpakana mtsogolo.

### **KUWONETSERA CHILANGO KWA MDANI:**

**...Mkuru wa dziko ili lapansi waweruzidwa. (Yohane 16:11)**

Pamene mukusanjika manja pa wodwala makhala mukulengeza kuti kalonga wa dziko lino waweruzidwa ndipo mphamvu ya madwale ndi matenda yaonongedwa. Kumbukirani kuti ndi mphamvu ya matenda yomwe yawonongedwa, osati kupezeka kwake. Tizaomboledwa kukupezeka kwake pamene tizakhala kwamphumfu mu Ufumu wa Mulungu.

### **KUDZUTSA ATSOGOLERI AUZIMU:**

Machiritso akhala akugwiritsidwa ntchito podzutsa atsogoleri auzimu, Paulo anayitanidwa kuti akhale mtumwi wa Uthenga Wabwino panthawi yakuchizidwa kwake (Machitidwe 9).

### **AMABWERETSA CHIMWEMWE CHACHIKULU:**

Werengani Machitidwe 8:5-25. Ndime imeneyi ikufotokoza za chimwemwe chachikulu chomwe chinabwera kwa anthu ndi madera omwe machiritso ndi mamasulidwe anatomikiridwa.

### **PAMENE MUKUYAMBA...**

Wolamulira wina wotchuka dzina lake Julius Caesar, anachirimika zogotsetsa Britain, anayenda panyanja ndi asilikali eka okwana zana limodzi (100) kuchoka ku France kupita ku Mangalandi. Kenako anatha ngalawa zomwe anagwiritsa ntchito kuolokera mtsinje wa English. Ndekunali kupita chitsogolo kukagonjetsa kapena kumfa. Panalibe mwayi obwerera.

Utumiki wa machiritso ndi mamasulidwe ndi waonse amene awotcha maulalo akusakhulupira ndi matha omwe alinao. Mutenga mbali ziwiri zokhudzana machiritso ndi mamasulidwe. Mukhala ngati Gamaliel, tsogoleri wa Chipangano Chakale, amene anayima pambali ndikupereka chenjezo. Anawauza atsogoleri ampingo kuti adikire ndi kuwona. Kapena akhale ngati Petro, amene anatenga ukaziwotche. Anachiza wolumala, kupalamula mkwiyo wa atsogoleri auzimu, ndiposo kutsutsana ndi atsogoleri amane anamuza kuti asalalikire kapenanso kuchiritsa mu dzina la Yesu.



Nthawi zonse kumbukirana, ndinu chotengera chachiritso, osati wochiritisa. Ndinu njira chabe imene Mchiritisi alimwainu amadutsiramo...

- Anthu amene amakumana ndizowawa koma amapirira ululu wake.
- Anthu amene azuzidwa ndi zomwe moyo wawachitira kapenanso amene atsadzidwa ndi chikumbu mtima chazomwe achita ndi moyo.
- Anthu amene akhumudwa, alibe chiyembekezo, ndipo akozekera kusalenda.
- Anthu amene ataya wokondedwa awo kapena avulazidwa ndipo mitima yao ikubuula ndi ululu, koma ndizawokha sangathe kuziwonetsera.
- Anthu amene amangidwa ndi magoli awuchimo ndi kumangidwa ndi satana.
- Anthu amene akumana ndi imfa.

Lingalirani funso iri lomwe Yesu anafunsa. “Chophweka nchiti, kunena kuti, ‘Machimo anu akhululukidwa’ kapena kunena kuti, ‘Dzuka, ndipo uyende?’

## MAYESO OZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera.

---

---

---

2. Fotokozani maganizo ena alipo pano okhudzana ndimachiritso.

---

---

---

3. Perekani mitundu isanu yamatenda.

---

---

4. Perekani tanthuzo la “machiritso akumwamba.”

---

---

---

5. Kodi gwero la matenda nchani?

---

---

6. Lembani zolinga zina zakudwala.

---

---

7. Kodi mathero awiri amathenda nchani?

---

8. Lembani zolinga zina zamachiritso akumwamba.

---

---

---

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

## ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Nawo ena mwa ma vesi oti mupitirize kuphunzirabe za machiritso ndi mamasulidwe. Akuphatikizapo malonjezano ndi zitsanzo zamachiritso ndi mamasulidwe.

### Umboni ochokera mu Chipangano Chakale

Genesis 17:18-19: Mulungu analonjeza kuchiritsa kusabereka kwa Sara.

Genesis 20:17: Mulungu anachiritsa Abimereki

Eksodo 4:6-7: Dzanja la Mose la khate

Eksodo 15:25-26 Mulungu awulula dzina lake ngati “Yehova-Rapha” kutathauza kuti “Ambuye wakuchiritsa.” Ana lonjeza kuti palibe nthenda iriyonse imene anaika pa Aaigupto imene izabwere pa Aaisreeli.

Levitiko 13:1-46: Mulungu analonjeza kuchotsa matenda pa anthu ake.

Levitiko 14:1-32: Malamulo okhudzana ndi khate

Levitiko 15:1-33: Malamulo amachiritso

Levitiko 16:29-30: Kuchiritsidwa kwamachimo

Numeri 12:1-15: Khate la Miriam ndi Aaron

Numeri 16:41-50: Muliri ukhudza Aisraeli

Numeri 21:5-9: Kuchiritsidwa kuchokera kuchifanifani cha njoka yamkuwa

Dueteronomo 7:15: Kumvera kwa Mulungu kumabweretsa moyo wathanzi

Dueteronomo 28: Matenda obwera chifukwa chosamvera Mulungu

Dueteronomo 29:22 Mulungu anaika matenda padziko

Dueteronomo 30:20: Mulungu ndi moyo ndi ochulukitsa masiku

Dueteronomo 32:39: Mulungu amakatha ndi kuchiritsa

Dueteronomo 7:15; 28:60: Matenda pa Aaigupto

Yoswa 5:8: Kuchiritsidwa kwachilengedwe kubala lamdulidwe

1 Samueli 6:3: Chopereka chopalamula chimabweretsa machiritso

1 Samueli 16:14-23: Mzimu woyipa umuzuza Sauli

1 Mafumu 5:23; 2 Mbiri 16:12: Matenda amapazi

1 Mafumu 8:37-40: Miliri mdziko

1 Mafumu 13:4-6: Munthu wadza lopuwala

1 Mafumu 17:17-24: Eliya aukitsa mwana kwa akufa. (Mtumwi ndi uthenga amatsimikizidwa chifukwa cha machiritso)

2 Mafumu 1:2; 8:8-9: Kodi ndizachira ku mnthenda imeneyi?

2 Mafumu 2:19-22: Kuchiritsidwa kwa madzi ndi Elisha

2 Mafumu 4:8-37: Kuukitsidwa kwa mwana waku Sunemu

2 Mafumu 5:1-14: Kuchiritsidwa kwa Namani

2 Mafumu 13:14,21: Elisa adwala nthenda yomutengera kuimfa

2 Mafumu 20:1-11: Kudwala kwa Hezekiya

2 Mbiri 6:26-31: Pemphero lakulapa ndi madwale

2 Mbiri 7:14: “Ndizachiritsa nthaka yawo”

2 Mbiri 16:12: Munthu wathenda yaikulu safuna Mulungu

2 Mbiri 20:9: Mulungu amava tikafuula muzowawa zathu

2 Mbiri 21:12-30: Nthenda yosachiritsika ya matumbo

2 Mbiri 24:25: Nthenda yotchulidwa kuti yauikulu

2 Mbiri 26:19: Khate la Uziya

2 Mbiri 30:20: Kuchiritsidwa kwa anthu ndi pemphero la Hezekiya

2 Mbiri 32:24-26: Kudwala kwa Hezekiya

Yobu 1-2: ma chaputala awa amawonetsa chiyambi cha mamvuto a Yobu, kuphatikizapo kudwala kwake

Yobu 5:18; 30:18: Yobu ayakhulapo za matenda ake

Masalimo 6:2-3: “Mulungu ndi chizeni”

Masalimo 27:1: “Mulungu ndiye mphamvu ya moyo wanga”

Masalimo 30:2: “Ndinafuula ndipo Inu munandichiza”

Masalimo 32:3-5 Kuvomereza tchimo kumabweretsa machiritso

Masalimo 34:19-20: “Zowawa za olungama ndi zochuluka, koma Mulungu amamulanditsa iye kwa iwo”

Masalimo 38:3,7: Mkwiyu ndi tchimo zimawononga moyo wanu; nthenda imatchulidwa kuti “chowoletsa”

Masalimo 41:1-8: “Chizani moyo wanga popeza ndakuchimwirani. “Nthenda ikutchulidwa kuti choipa”

Masalimo 42:11; 43:5: Mulungu ndi thanzi wanthu

Masalimo 55:1-2: Kuchiritsidwa kwa mzimu wakugwa

Masalimo 60:2: “Kuchiza kwazolakwa zadziko”

Masalimo 67:2: “Kuti njira zanu zidziwike pa dziko la pansu, kupukulutsa kwana kochiza pakati pa mafuko”

Masalimo 72:13: Ndife ofooka ndi chisoni

Masalimo 91:9, 10: “Palibe mulire omwe uzafike komwe umakhala”

Masalimo 103:1-5: “Osaiwalira zomwe wakuchitira... Ndiamene wachiritsa nthenda zako zonse”

Masalimo 105:37: Israeli anabwera wabwinobwino opanda modzi yemwe ovulala. Anthu okwana 3,000,000 onse anali bwino ndi amphamvu.

Masalimo 107:17-20: “Anatumiza Mau Ake ndipo anachiritso iwo”

Masalimo 119:25-28: Timalimbikitsidwa ndi Mau

Masalimo 119: 67: “Poyamba nazuzidwa, ndipo nasochera”

Masalimo 147:3: “Amene amachiza nthenda zako zonse.” Machiritso amtima osweka.

Masalimo 105:37: “Anatulutsa onse...Palibe ndi modzi yemwe amene anamwalira.

Miyambo 3:7-8: Mmene tingakhalire moyo wathanzi

Miyambo 4:20-23: Zinthu zokhudzana moyo zimasokonekera ndi zamuntima. Malonjezano a Mulungu ndi moyo kwa onse amane awapeza ndipo ndi nthanzi kunthupi lawo.

Miyambo 12:18: Lirime la munthu wa nzeru limabweretsa machiritso

Miyambo 13:17: Kazembe wokhulupirika amafanizidwa ndi moyo wathanzi

Miyambo 15:4, 30: Lilime lowongoka ndi moyo; uthenga wabwino umakoza moyo

Miyambo 16:24: Mau a Mulungu amabweretsa moyo kumafupa

Miyambo 17:22: Mzimu wosweka omasokoneza mafupa

Mlaliki 3:3: Pali nthawi yake yochiza

Mlaliki 17:22: Chisoni ndi mkwiyo zimabweretsa matenda

Yesaya 6:10: Kumvetsetsa kukambira, machiritso

Yesaya 19:22: Pamene Mulungu wapephedwa, Amachiritsa

Yesaya 33:3-4: Uneneri wamachiritso kukhala mbali imodzi ya Ufumu wa Mulungu

Yesaya 35:5-6: Machiritso m'tsogolo

Yesaya 38:1-12: Kudwala kwa Hezekiya ndikubwerera kwake kumoyo wathazi

Yesaya 53:5: Talonjezedwa machiritso ndi mamasuridwe kupyolera mu imfa ya Yesu

Yesaya 57:18-19: Senderani chifupi ndimachits

Yesaya 58:8: Machiritso azatumphuka

Yesaya 61:1: Yesu anatumidwa kuti azamange mitima yosweka

Yeremiya 3:22: Mulungu amachiritsa onse obwerera m’mbuyo

Yeremiya 8:14-15; 20-22: Nthawi yamachiritso. Ululu wa tchimo umakhudza nthanzi lo la thupi

Yeremiya 15:18: Mmene tingathanirane ndi matenda osachizika

Yeremiya 14:19: Kodi palibe machiritso anthu?

Yeremiya 17:14: “Ndichizeni ndipo ndizachiritsika”

Yeremiya 30:12-17: Mulungu azabwezeretsa nthazi

Yeremiya 33:6: “Ndizachiritsa iwo”

Yeremiya 46:11: “Palibe kuchira kwawo”

Yeremiya 51:8-9: Kuchiritsidwa kwa Babulo

Maliro 2:13: “Ndindani amene angachiritso inu”

Maliro 2:33: “Mulungu samalanga mofuna”

Ezekieli 14:19: “Kodi kulibe machiritso anthu?”

Ezekieli 17:14: “Ndichizeni ndipo ndizachizika”

Ezekieli 30:17: “Zabwezeretsaso nthanzi”

Ezekieli 30:12-13: Zilonda zosachiritsika makhwala sangachiritse

Ezekieli 30:21: Chomwe Mulungu waphwasula palibe yemwe angachiritse

Ezekieli 33:6: “Ndizawachiritso iwo”

Ezekieli 34:4, 16, 21: Chenjezo kwa abusa omwe sanachiritsidwe

Ezekieli 47:8-12: Kuchiritsidwa kwa madzi

Danieli 4:34,36: Kuchiritsidwa kwa Nebukatineza

Hoseya 5:13: Kupita kwina chifukwa chamachiritso. Munthu sangachiritse bala lobweretsedwa ndi Mulungu.

Hoseya 6:1: “Yense yemwe wang’ambika ndipo Iye azamuchiza”

Hoseya 7:1: Machiritso kwa Aaisraeli

Hoseya 11:3: “Samazindikira kuti Ndinawachiritsa”

Hoseya 14:4: “Zachiritsa kubwerera mbuyo kwawo”

Nahumu 3:19: Nyengo yowawitsa

Zakariya 11:16: Chenjezo kwa abusa omwe samachiritsa

Malaki 4:2: Machiritso mmapito Mwake

## UMBONI WAMU CHIPANGANO CHATSOPANO

Mateyu 8: 13: Malo okumanirana amaika nthawi

Mateyu 8:17: Yesu anasenza matenda athu

Mateyu 10:1: Mphamvu pa matenda ndi ziwanda zapatsidwa kwa okphunzira Ake

Mateyu 18:19-12: Pomwe awiri amvomerezana amalandira chomwe apempha

Marko 2:17: Khristu anabwera kuzachiritsa ochimwa

Marko 3:15-17: Khristu anapereka mphamvu yochiza odwala

Marko 4:18-19: Kuchiritsa inali mbali imodzi yakudzodzedwa kwadzedwa kwa Yesu ndipo anatomizidwa kuzachiritsa

Marko 11:24: Ngati tikhulupirira pamene tipemphera (osati mukalandira), muzalandira.

Marko 16:18: Mudzina la Yesu okhulupirira azachiritsa ndi kutulutsa ziwanda

Luka 5:31: Odwala amafuna sing'anga

Luka 7:6: Kusayenera kunawonekera ndi Yesu ngati chikhulupiriro

Luka 17:6: Chikhulupiriro chochepa chikhoza kubweretsa zotsatira zazikulu

Luka 18:7-8: Musamasiye yankho lanu lisanafike

(Nkhani ya Danielo mu Chipangano Chakale imawonetseraso kupambana kwapemphero: Mulungu anamumva Danielo patsiku loyamba lomwe, koma satana anagwirigwira kwa masiku 21)

Yohane 6:53-58: Nthupi ndi mwazi wa Yesu umabweretsa moyo

Yohane 10:10: Yesu anabwera kuti tikhale ndi moyo. Satana anabwera kuzampha, kuba ndi kuwononga

Yohane 11:1-45: Nthenda yosachizika pano imapereka njira kuchozizwa chapamwamba

Yohane 15:7: Ntchito zimene Yesu anachita, tikuyenera kuzichitanso

Yohane 16:24: Pemphani mu dzina Lake ndipo muzalandira.

Aroma 2:4: Chifundo cha Mulungu chimatsogolera kukulapa. (Dziwani kuti matenda satsogolera kukulapa; ndi kukoma mtima kwa Mulungu basi)

2 Akorinto 4:16: Munthu wanthu wakunja amawonongeka, koma munthu wamkati akhoza kukozedwaso

Aefeso 3:20-21: Mulungu ali ndimphamvu yogwira ntchito mwa ife pazonse zimene timapempha kapene kuganiza

Afilipi 2:25-27: Kudwala kwa Epafrodito

Akolose 4:14: Luka, sing'anga, anali mbali imodzi ya Paulo kufalitsa Uthenga

2 Timoteo 4:20: Trofimo nkhani yake irimwachidule, zochepa zokha ndizimene zingapezeke kuchokera muzimenezi. Paulo sikuti anamusiya akudwala, koma sitinauzidwe ngati anachiritsidwa pompo kapena pang'onopang'ono, kapena kuti chinaretsa machiritso ake nchani.

Ahebri 4:15: Amakhudzika ndi zowawa zanthu

Ahebri 11:1: Chikhulupiriro ndiumboni wa zinthu (machiritso) zosawoneka

Yakobo 1:6: Tikuyenera kupempha ndi chikhulupiriro osati kugwedezeke

Yakobo 1:17: Mphatso ina iriyonse yabwino (machiritso) imachokera kwa Mulungu

Yakobo 5:14-15: Kuitana akulu ampingo kuzakudzodzi ndi mafuta, pemphero lachikhulupiriro, machiritso ndi kukhululuka

1 Petro 2:24: Tinachiritsidwa ndi mabala Ake

1 Yohane 3:22: Chilichonse tipempha tikhoza kulandira ngati tiriomvera

3 Yohane 1:2: Moyo wanthazi umagwirizan ndi nyengo ya moyo wanu

Marko 7:36; 8:26; Mateyu 8:4: Musamaseweretse machiritso

Chibvumbulutso 20:2-3: Pamene satana azamangidwa, sipazakhalanso matenda ndi imfa

Chibvumbulutso 21:4: Machiritso omaliza: Sikuzakhalanso machiritso ndi imfa

2. Mulungu walonjeza machiritso ndimamasulidwe. Nawo ena mwa ma vesi okhudzana ndi malonjezano a Mulungu:

**Unthenga Wabwino ndi mphamvu kwa wina aliyense amene akhulupirira.  
(Aroma 1:16)**

**Malonjezano a Mulungu ali... “moyo kwa onse omwe atawapeze, ndi thanzi kumatupi awo.” (Miyambo 4:22)**

**Popeza malonjezano onse a Mulungu ali mwa Iye ndi ( inde) ndi amene (akhale choncho) ku ulemerero wa Mulungu kwa ife. (2 Akorinto 1:20)**

3. Umu ndimomwe mphatso zina za uzimu zmigwiritsidwira ntchito mogwirizana ndi mphatso ya machiritso
  - Kuphunzitsa ndi kulimbikitsa: Kochokera mMau, zimakuza chikhulupiriro chamachiritso
  - Uneneri, Malirire, kumasulira: Kumabweretsa Mau ochokera kwa Mulungu okhudzana machiritso
  - Kuzindikira mizimu: Kuzindikira mizimu yomwe ikugwira ntchito ndikuwulula ngati machiritso kapena mamasulidwe akufunika.



- Mphatso ya chikhulupiriro: Imapereka kulimbika kwapaderadera ku chidziwitso chozindikira ndi kupemphera pemphero la chikhulupiriro.
- Mau anzeru: Amapereka chidziwitso wachoyambitsa cheni cheni cha nthenda. Imathandizira machiritso amkati kapena ngati machiritso akuthupi akugwiririzana ndi mavuto a ziwanda. Amatha kupereka chidziwitso chokhudzana ndi machimo omwe akuyenera kulapidwa, mphamu ya ziwanda ikukhudzidwa, ndipo zamalingaliro zimene zimatchinga machiritso ndizina zotero.
- Mphatso ya zozizwa: Machiritso apompopompo komakulenga monga, kumera kwa nthiti, ndizina zotero. Pali zochitika zoti sizingafotokozedwe mwanjira ina iriyonse yachirengedwe, ndizithu zoti sizingafotokozedwe mwachilengedwe.

*Kuti muphunzire zambir za mphatso zauzimu, pezani buku la sukulu ya Harvestime International lotchedwa kuti “Utumiki wa Mzimu Woyera.”*

4. Mau azozizwa: Kulandira zozizwa, mukuyenera kulandira kaye panoka, mphamvu ya kumwamba imene ndi yayikulu kuchilengedwe ndipo muzikwanitsa kuyilamulira. Mphamvu imeneyo ndi Mulungu. Zozizwa ndi mabvumbulutso ochokera kumwamba. Mulungu analenga momwe zinthu zimayenera kukhalira, koma Iye samaletsedwa ndi izo.

Kuchiritsidwa mozizwitsa ndikubwezeretsedwa ku ugwiro. Ndi imfa, osati kuukitsidwa, izi sizachiringedwe. Ndi nthenda ndi kugwidwa ndi ziwanda zomwe zimasokoneza malamulo achilengedwe cha Mulungu. Nde zhozizwa chamachiritso, mamasulidwe, ndizina zotero., ndikubwereranso ku moyo wagwiro.

## CHAPUTALA 17

### ZOCHITIKA ZOMWE ZIMASOKONEZA MACHIRITSO

#### ZOLINGA:

Pomaliza paphunziroli mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera wosawonera.
- Kupereka tanthauzo la “machitachita.”
- Kufotokoza zikhalidwe zina za munthu zomwe zimasokoneza machiritso.
- Kufotokoza machitachita ena omwe amasokoneza machiritso.

#### VESI YOTSOGOLERA:

**Kuti njira yanu idziwike pa dziko lapansi, Cipulumutso canu mwa amitundu onse. (Masalmo 67:2)**

#### CHIYAMBI

Nchifukwa chani anthu ambiri samachiritsidwa? Nchifukwa chani ena amachiritsidwa pamene ena ayi? Nchifukwa chani akhristu amene ali osazikika kwambiri ndi achikunja amachiritsidwa pamene anthu amene ali owongoka komaso owona mtima ndi ozipereka sanalandirepo machiritso? Awa ndi ena amwamwa funso amene muzalandire pamene mwayamba kutumikira machiritso ndi mamasulidwe. Phunziro lino likukhudza machitamachita amene amasokoneza machiritso. Mchitidwe ndi chochitika chimene chamapangitsa kuti pakhale kusiyana kapena zotsatira zosiyana.

Mulungu analonjeza machiritso mmau Ake. Tikuyenera kukumbukira, kuti lonjezano lirironse la Mulungu lilindi malire mmene munthu angavomerere. Ichi nchifukwa chake nkoyenera kumvetsa bwino machitamachita omwe angaononge machiritso.

#### KUMVETSETSA NDI KUTHANA NDI MACHITACHITA

Machitachita mu utumiki wa machiritso ndi zifukwa zomwe anthu ena amachiritsidwira pamen ena ayi. Musanayambe phunziro ili, mkofunika kukumbukira kuti simuzakhala ndi mayankho afunso lilironse lomwe muzakumane nalo pa machiritso ndi mamasulidwe.

Ndichikhalidwe cha munthu chofuna kumvetsetsa chilichonse. Yeselo loyamba linakhazikika pa nkhani imeneyi. Khumbokhumbo lofuna kudziwa zinthu zonse limachokera kuukira pokhala ndi mafunso opanda mayankho. Mvuto limeneri lomwe munthu alinalo ndilomwe mukuyenera kuligonjetsa kuti mukakwanitse kutumikira machiritso ndimamasulidwe mwapindula. Baibulo limaulula mwamachitachita ena omwe amasokoneza machiritso ndi mamasulidwe, koma simudzakhala ndi mayankho pamafunso onse. Ngati mutero, simuzafunanso Mulungu kapena chikhulupiriro. Baibulo lilichindunji kuti zinthu zina ndizoululika kwa ife, pamene zina ayi:

**Zinsinsi nza Yehova Mulungu wathu; koma zobvumbuluka nza ife ndi ana athu kosatha, kuti ticite mau onse a cilamulo ici. (Deuteronomo 29:29)**

Mumachiritso ndimamasulidwe, mukuyenera kuphunzira kuyika pambali mafunso opanda mayankho, ndikusiyira Mulungu zinthu zonse zachinsisi.

Machiritso ndi mamasulidwe zirimbali ya Uthenga Wabwino monga ngati mmene chiririnsu chipulumutso. Pamene mukutumikira machiritso ndi mamasulidwe ndipo ena sanalandire, muzayedwe kuti mungosiya. Koma lingalilani funso ili: Kodi masiya kulalikira chipulumutso chifukwa aliyense wamva Uthenga sanapulumsidwe? Nde nchifukwa chani mathamangira kuleka kutumikira machiritso ndimamasulidwe chifukwa aliyense sanalandire? Nchifukwa chake nthawi zambiri mmachiritso ndi mamasulidwe, kunyada kumalowapo. Timachita manyazi pomwe tapepherera munthu amene akudwala mowoneka ndipo sanachiritsidwe. Ena amatha kuwona chifukwa ndizakunja. Ngati wina avomera chipulumutso koma sanapulumsidwe, anthu sangawone chifukwa ndizamkati. Kunyada kwanthu kumakhudzidwa ndizomwe anthu amawona kunja.

Simuzakhala ndi mayankho azochitika zonse zomwe zimasokoneza machiritso monga ngatinso zochitika zina zomwe zimasokoneza chipulumutso. Ena amapulumsidwa, ena ayi. Ena amachiritsidwa, ena ayi.

Baibulo limaulula mwa zina mwazochitika zomwe zimasokoneza machiritso ndimamasulidwe. Ndikofunika kwambiri kumvetsa zimenezi kuti mukathe kuthandiza ena kuti athane nazo kuti akathe kulandira machiritso. Nao machitachita amenewa:

### **KUSOWA CHIPHUNZITSO**

Kusowa chidziwitso chokhudza machiritso, ndondomeko zake, kochokera, mmene tingawiritsire ntchito chikhulupiriro, ndi mmene tingalandirire zimasokoneza machiritso. Mulungu anati:

**Anthu anga akuonongeka chifukwa chosadziwa. (Hoseya 4:6)**

Yesu anati timalakwitsa ngati sitikumvetsa mau a Mulungu ndi mphamvu Yake.

**Koma Yesu anayankha, nati kwa iwo, Mungolakwa a osadziwa malembo, kapena mphamvu za Mulungu. (Mateyu 22:29)**

Anthu ena salandira machiritso chifukwa samavetsa mau a Mulungu ndi mphamvu Yake.

Chikhulupiriro chamachiritso chimabwera pakumva Mau a Mulungu okhudzana ndi machiritso (Aroma 10:17). Baibulo limawatchula Mau a Mulungu kuti mbeu. Anthu ena amayesera kukolola kholola la machiritso popanda mau amachiritso kubzalidwa mmitima mwao. Mbeu singawire ntchito ngati sili mwaife. Asananene kuti “Ndine Mulungu amene ndimachiza,” Mulungu koyamba anati, “Ngati azakhazikika Mmau anga.” Mau amabweretsa machiritso.

Ndi anthu angati omwe angapulume ngati sanamve Uthenga Wabwino wa chipulumutso? Kapena ndi angati omwe angapulume ngati mfundo zikulu zikulu za chipulumutso uthenga wake unali:

- Mwina sichifuniro cha Mulungu kukupulumutsani.
- Machimo anu ndi amabweretsa ulemero kwa Mulungu.
- Tsiku lachipulumutso linali lakale.

Ngakhalenso timamva mayakhulidwe okhudzana ndimachiritso omwe ndimbali imodzi yomwe Yesu anaziperekerera:

- Mwina sichifuniro cha Mulungu kukuchizani.
- Matenda anu ndi ulemero wa Mulungu.
- Masiku amachiritso anapita kale.

Anthu akuyenera kuphunzitiwa Mau a Mulungu okhudzana ndi machiritso monga ngati momwe amaphunzitsidwira chipulumutso. Ndi mbeu ya Mau a Mulungu yomwe imabweretsa machiritso.

### **CHIKHALIDWE CHA ANTHU**

Chikhalidwe ndi zikhulupiriro, malamulo ndi mfundo za munthu. Chikhalidwe ndi zikhulupiriro zanthu zimatchinga ntchito ya Mau a Mulungu.

**...Ndipo inu mupeputsa mau a Mulungu cifukwa ca miyambo yanu. (Mateyu 15:6)**

Ngati chikhulupiriro chimabwera pakumva Mau a Mulungu, ndekuti chikhoza kuchokosa pokumva ndi kumvomera chikhalidwe ndi chiphunzitsa cha munthu chomwe chimawononga chikhulupiriro. Nazo zikhalidwe za munthu zomwe zimasokoneza machiritso:

#### **CHIKHALIDWE CHIMATI:**

“Machiritso ndi zozizwa zizalero.”

Anthu ena amanena kuti machiritso anali anthawi ya Baibulo basi kapena ndi amtsogolo pakubweranso kwa Yesu.

#### **KAMVOMEREDWE KANTHU:**

Mulungu anati:

**... pakuti Ine Yehova ndine wakuciritsa iwe. (Eksodo 15:26)**

“Ine Ndine” akukamba za lero. Ndetisithe bwanji kukhala “Nalipo” kale kapena “Zakhalapo” mtsogolo? Baibulo limaphunzitsa kuti Mulungu samasitha.

**Mphatso iri yonse yabwino, ndi cininkho ciri conse cangwiro zicokera Kumwamba, zotsika kwa Atate wa mauniko, amene alibe cisanduliko, kapena mthunzi wa citembenukiro. (Yakobo 1:17)**

**Pakuti Ine Yehova sindisinthika... (Malaki 3:6)**

Mulungu sanasithepo chiyambireni:

**Musaumitse mitima yanu, monga m'kupsetsa mtimamo, Monga muja tsiku la ciyesero m'cipululu. (Ahebri 3:8)**

Ngati tsiku la chozizwa linali lakale, ndekuti ziri chimodzi modzi ndi tsiku lachipulumutso, popeza palibe chozizwa chopambana kuposa chipulumutso. Ena amati machiritso nsi atsogolo pamene Yesu azabwerenso kudziko lapansi. Ngati izi zilizowona, ndekuti utumiki wa aphunzitsi, abusa ndi atsogoleri ena ukuyenera kukhala wa nthawi yakutsogolo chifukwa mphatso yamachiritso ndi mphatso ya uzimu chimodzimodzinso mphatso zinaso.

Yankho lomveka bwino kuchitsutso chonena kuti zozizwa sizamasiku ano ndi zolembedwa zomwe zinachitika. Yesu anachita zozizwa ndi kuchiritsa:

**Ndipo anayankha, nati kwa iwo, Mukani, muuze Yohane zimene mwazona, nimwazimva; anthu akhungu alandira kuona kwao, opunduka miyendo ayenda, akhate akonzedwa, ogontha akumva, akufa aukitsidwa, kwa aumphawi ulalikidwa Uthenga Wabwino... (Luka 7:22) Onaniso Machitidwe 4:14-16**

Buku la Machitidwe linalimba zozizwa ndi machiritso mu mpingo woyamba. Zolembaso zatsopano zokhuna ndi mbiri ya mpingo zimavomerezaso za machiritso ndi zozizwa zambiri. Anthu ena amafusa, “Ngati machiritso ali alero, nchifukwa chani okhulupira samayendayenda kumachiza odwala ndi kuukitsanso akumfa?” kuukitsa akumfa sinali mbali yakutumidwa kwakukulu komwe kunaperekedwa ku mpingo. Kunalamuliridwa kwa ophunzira pamene anatumizidwa kuyamba kukalengeza Ufumu. Kuukitsa akumfa chinali chipatso choyamba chakuuka kwa Yesu chomwe chimayenera kuti chizachitike.

Pali kusiyana pakati pa zozizwa zapaderadera ndi zozizwa zapangano. Zozizwa zapaderadera zinachitika monga ngati chizindikiro munyengo yapaderadera, monga ngati kusitha madzi kukhala vinyo, kuyenda panyanja, kuchulukitsa mkate ndi nsomba, kutsekula Nyanja yofila, ndikuukitsa akumfa. Machiritso ndi chozizwa chapangano la mu Chipangano Chakale, osati chizozizwa chapadera. Mulungu akuukitsabe akumfa, koma izi zimachitika malingani ndi mphamvu Zake ndipo siziri mbali imodzi yakutumidwa kwanthu kukachiza.

Tinakalibe pa phunziro la imfa, anthu ena amanena kuti ngati machiritso akumwamba amagwiradi ntchito, ndekuti sipanakakhala Kristu yemwe akamafa. Maganizo awa sananenedwe mmalemba. Baibulo limapereka umoyo wathanzi wochokera kumwamba munyengo yomwe munthu alindi moyo.

Ngakhale imfa ya Yesu inatigulira chiwombolo chamuyaya kuchokera ku imfa, komabe matupi anyamawa azamfabe kupatula ngati Yesu angabwere nsanga ndikuti mkwatulo uzachitike. Baibulo lomwelo lomwe limaphunzitsa zamachiritso linayikaso malire amoyo wa munthu.

**Masiku a zaka zathu ndiwo zaka makumi asanu ndi awiri... (Masalmo 90:10)**

**Ndipo popeza 8 kwaikikatu kwa anthu kufa kamodzi, ndipo 9 atafa, ciweruziro. (Ahebri 9:27)**

### **CHIKHALIDWE CHIMATI:**

“Munthawi ya Yesu kunalibe chinthandizo chamakhwala chodalilika. Koma tsopano nthandizo lilipo, tikuyenera kuligwiritsa ntchito mmalo mopephera kwa Mulungu kufuna machiritso.”

### **KUYAKHA KWATHU:**

Kuchokera kalekale muzaka za ma 400 B.C, kunali ukadaulo wamakhwala wochiritsa. Hippocrates mu zaka ma 460-370 B.C, tate wa zamakhwala, anapanga ukadaulo wazamakhwala omwe unali wapamwamba kwambiri. Wina waukadaulo wake

ukugwiritsidwabe ntchito mpakana lero. Greece, Egypt, ndi Rome anali ndi akadaulo azamakhwala mu nthawi ya Yesu.

Machiritso akumwamba sakhudzana ndi ukadaulo kapena kupanda ukadaulo pa zamakhwala. Ndi mdalitso omwe unaperekedwa mu imfa ya Yesu. Mphatso ina iriyonse yabwino imachokera kwa Mulungu, nde mkololedwa kugwiritsa ntchito makhwala ovomerezeka. Kumbukirani kuti makhwala simulowa mmalo alonjezano lapangano la machiritso.

Ngakhale kuti ntchito zamakhwala zikupita patsogolo komabe pali matenda ambiri osachiritsika, nde machiritso akumwamba ngofunikabe. Komanso anthu ambiri samatha kufikira mtengo wamakhwala. Mwachitsanzo, mu Afrika zadziwika kuti anthu okwana 80% samalandira nthandizo lamakhwala.

### **CHIKHALIDWE CHIMATI:**

“Machiritso akumwamba amaphunzitsidwa ndi zipembedzo zonyenga.”

### **KUYAKHA KWATHU:**

Wesley, Luther, ndi Zinzendorf ampingo wa Methodist, Lutheran, ndi Moravian, onse anaphunzitsa zamachiritso ochokera kumwamba. Onse amene amaphunzitsa lero, pamodzi ndi mphamvu yopulumutsa ya mwanzi wa Yesu ndi Umulungu wa Khristu, salinso ovomerezeka ngati atsogoleri amenewa. Zipembedzo zina zonyenga, zimaphunzitsa machiritso koma simachiritso eni eni omwe Baibulo limaphunzitsa.

Satana ndi wonyenga ndi wokopera. Sitingachotse machiritso akumwamba chifukwa wanyenga ndikuchiza kupyolera mu mphamvu yoyipa. Satana akunyenga ambiri kuti akhulupirire kuti mtsinje wa Ganjes ku India ungawayeretse machimo awo. Kodi tileke kulalikira chipulumutso chifukwa satana akukopera? Choonadi nchakuti ngati satana akukopera machiritso akumwamba ndendichizindikiro chakuti pali machiritso owonadi.

### **CHIKHALIDWE CHIMATI:**

“Mazunzo awolungama ndi ochuluka. Matenda anu ndi chizunzo mukuyenera kukhala nawo chifukwa ndinu olungama.”

### **KUYAKHA KWATHU:**

Tanthauzo la mau akuti “chizunzo” omwe agwiritsidwa ntchito pa Masalimo 34:19, komwe chikhalidwe chimenechi chinachokera, sichimatanthauzo matenda, koma kuyesedwa, zowawa, chizunzo, kapenaso mayenselo. Ngakhale kukhala kuti amatanthauza kuti matenda, chomwe vesiyi ikutikumbutsa nchakuti Atate akufuna kutipulumutsa.

Pa Yakobo 5:13-16 paperekedwa kusiyandwa kwa zowawa ndi matenda. Kodi wina wa inu akumva zowawa? Apemphere (Yakobo 5:13). Ngakhale mungapephe ena kuti akupephe nanu limodzi, sikuti ali ndi udindo opempherera mabvuto anu onse kuti achoke.

Malemba akulamulirani kuti mupemphere pamene mukumva zowawa chifukwa mukuyenera kuphunzira kukhala ogonjetsa kupyereka pakupemphera nokha mukakhala muzowawa ndi mayesero. Mu nthawi yakudwala, akulu ampingo akuyenera kuitanidwa kuzapemphera (Yakobo 5:14). Wodwala akuyenera kupulumutsidwa (kunthenda yakunthupi), kudzudzitsa (Kubwezeretedwanso mphamvu), ndikukhulukiridwa machimo awo (Machiritso auzimu).

## **CHIKHALIDWE CHIMATI:**

“Nthenda yanu ndi ‘minga mthupi mwanu’ monga Paulo kapena ndi mtanda wanu. Mukuyenera kuphunzira kukhala nayo.”

## **KUYAKHA KWATHU:**

Kunena kuti thenda ndi mtanda wanu ndizothana nazo mophweka. Mtanda simamvuto, matenda ndi zowawa zomwe zimabwera kwa ife popanda kusakha kwathu. Yesu ananena moveka bwino kuti “kunyamula mtanda” ndimchitidwe ozipereka, osati timangovomera chifukwa tiribe kusakha. Yesu sananene kuti matenda ndi imfa ndi mtanda wochokera kwa Mulungu. Anane kuti ziringati adani.

“Minga m’thupi” kuyekhula kumeneku kumatsamira pa minga yomwe inali m’thupi mwa Paulo zomwe zinalembedwa pa 2 Akorinto 12. Anthu amene amakhulupirira kuti minga ya Paulo anali matenda amanena mfundo yofunika akamakamba za machiritso. Okhulupirira ambiri anyengedwa osalandilaso machiritso chifukwa chachiphunzitso chaminga ngati chiphunzitso chamatenda.

Tiyeni tiwone zimene Malemba amanena zokhudzana ndi minga imeneyi.

## **Kodi inali chani:**

Baibulo limanena kuti “anali wantenga.” Pa Chigriki liwu loti “wanthenga” limawoneka kasanu ndi kawiri mu Chipangano Chatsopano. Linamasuliridwa kuti “mngelo” linagwiritsidwa ntchito nthawi kwa 181. Nthawi zonsezi limakamba za umunthu, osati matenda kapena madwale. “wanthenga” ndi munthu.

## **Kodi inachokera kuti:**

Baibulo limati inali wa nthenga wa satana.

## **Nchifukwa chani inalolezedwa:**

Paulo anati minga imeneyi inalolezedwa chifukwa chamabvumbulutso ochuluka amene analandira komanso chifukwa chachikhalidwe chake chozitamandira. Munthu wina aliyense asanayambe kunena kuti alindi minga nthupi aziyamba kaye walingalira kuti kodi ndi mavumbulutso ndi masomphenya angati amene alinawo. Kodi akukwanira kukhala ndi minga? Anthu ambiri amene amaganiza kuti alindiminga m’thupi mwawo amakhala kuti alibe bvumbulutso ndi masomphenya.

Minga inalinso mbali imodzi yokwaniritsa uneneri. Pamene Paulo anatembenuka mtima, Mulungu anati:

**...Pakuti Ine ndidzamuonetsa iye zinthu zambiri ayenera iye kuzimva kuwawa cifukwaca dzina langa. (Macitidwe 9:16)**

## **Zomwe inachita:**

Minga inamuzusa Paulo. “Kuzuza” kumatanthauza kuti kmenya mobwereza, kabwerezabwereza. Mau oti “kuzuza” sakutanthauza kuti nyengo ya matenda yokhazikika koma kumenya mubwereza. Wanthenga anatumidwa kukamusautsa Paulo pofuna kuletsa Mau a Mulungu kuti asalalikidwe.

Mulungu sanalonjeze kuchotsa kuzuzika kwa okhulupirira, koma analonjeza kuchotsa matenda awokhulupirira. Malemba atichenjeza kawirikawiri kuti ngati tikhala mowonadi mtima tizalandira chizuzo ndimasautso, koma osati matenda.

### **Kodi inawonetseredwa bwanji:**

Nazo zina mwazitsanzo zomwe mimga inatumphutsira chotsutsa kwa Paulo:

- Ayuda anafuna kumupha Paulo atangotembenuka mtima kumene: Machitidwe 9:23
- Paulo analetsedwa kukalumikizana ndi okhulupirira ena: Machitidwe 9:26-29
- Anatsutsidwa ndi satana: Machitidwe 13:6-12
- Anatsutsidwa ndi Ayuda pachimpwirikiti: Machitidwe 13:44-49
- Anapirikitsidwa ku Antiokya wa m'Pisidiya: Machitidwe 13:50
- Anamenyedwa ndikupitikitsidwa ku Ikoniyo: Machitidwe 14:1-5
- Anathawira ku Lustra ndi Derbe komwe anakagendedwa ndipo anasiyidwa ngati wamfa: Machitidwe 14:6-19
- Anatsutsidwa kwambiri ndi abwenzi onyenga: Machitidwe 19:8
- Anamenyedwa ndi kuikidwa mndende ku Filipi: Machitidwe 16:12-40
- Anamenyedwa ndikupitikitsidwa ku Tesalonika: Machitidwe 17:1-10
- Anamenyedwa ndikupirikitsidwa ku Bereya: Machitidwe 17:10-14
- Anamenyedwa ku Korinto: Machitidwe 18:1-23
- Anamenyedwa ku Aefeso: Machitidwe 19:23-31
- Ayuda anampangira chiwembu chofuna kuchotsa moyo wake: Machitidwe 20:3
- Anagwidwa ndi Ayuda, anazuzidwa, kuyesedwa kumabwalo amilandu kasanu, ndiposo anamva zina zowawa zambiri: 2 Akorinto 11:23-33

Palibe olo pamodzi, muzolembedwa zake, pamene Paulo anatchula matenda kukhala chizunzo chimene chinamuzuzika. Mu 1 Akorinto 4:11, Paulo anawonetsera kuti lingaliro lake lakuzuzika silinali lokhazikika ngati matenda. Anati, “Kufikira nthawi yomwe yino timva njala, timva ludzu, tiri amaliseche, tikhomedwa, tiribe pokhazikika.” Paulo anadwalapo monga mmene zinalembedwera pa Agalatiya 4:13-16, koma iyi sinali minga yake chifukwa sinali nyengo yokhalitsa. Anati anadwala kumayambiriro kokha.

Ena amakhulupirira kuti minga ya Paulo inali diso lang'ala, koma maso ake anachiritsidwa ku khungu (Machitidwe 9:18). Kupitiriza kukhulupirira kuti anali ndi mvuto la maso zimatsutsana ndi mphamvu yamachiritso Amulungu. Komaso, kodi kunakakhala kwa bwino kunena mvuto la diso kuti linabwera chifukwa chowona ulemmerero wa Mulungu kukhala wanthenga wa satana? Paulo mwini wake amatiuza kuti muchaka cha 60 A.D, pamene analemba kalata yake, panali patapita zaka 14 chilandirireni mabvumbulutso ochulukana amene anabweretsa minga nthupimwake. Panali patatha zaka 12 chitembenukirireni mtima pamene anawona ulemmerero wa Mulungu.

### **ZOTSATIRA ZAKE:**

Paulo anayakhulapo za mazunzo ake kutanthauza kuti “amkasowa mphamvu, kufooka, kulephera kubweretsa zotsatira kupyolera mukuyesa yesa kwake.”



Chimaliziro chokhudzana ndi minga ya Paulo ndichakuti sitingadziwe bwino bwino kuti mingayo inali chani, ngati munaphunzidwa kuti anali matenda kumbukira izi maganizo mwanu:

Minga ya Paulo inawonetsera mphamvu ya Mulungu mmoyo mwake. Anthu ena amagwiritsa ntchito “minga mthupi” pofuna kuzimbaita kumatenda. Akuyenera kuzindikira kuti zitsanzo za m’Baibulo zoterozo zinatsutsidwa ndi anzake omwe amayenda nawo mu utumiki. Minga sinamuletse kugwira ntchito mu Ufumu wa Mulung kapena kuwonetsera mphamvu ya Mulungu kupyolera mwa iye.

### **KUSAKHULUPILIKA**

Chochitika china chomwe chimasokoneza machiritso ndi kusakhulupirira. Kusakhulupirira kukhoza kuchokera ku...

- Kuganiza kuti Mulungu sangachize.
- Kuganiza kuti Mulungu angachize, koma akhoza kusakha wosandichiza ine.
- Kuganiza kuti Mulungu angachize, ndipo akuyenera kundichiza, koma osati pano.
- Zotizungulira zomwe zimabweretsa kusakhulupirira zomwe zimaletsa machiritso.

Pali zitsanzo zambiri m’Baibulo za zomwe kusakhulupirira kumatchingira ntchito ya Mulungu. Mu mzinda wa Nazaleti Yesu...

**Ndipo Iye, cifukwa ca kusakhulupirira kwao, sanacita kumeneko zamphamvu zambiri. (Mateyu 13:58)**

Yesu anazizwa, kapena kudabwa, kuti anthu sanakhulupirire:

**Ndipo anazizwa cifukwa ca kusakhulupirira kwao... (Marko 6:5-6)**

Baibulo limati:

**Koma apemphe ndi cikhulupiriro, wosakayika konse; pakuti wokayikayo afanana ndi pfunde la nyanja lotengeka ndi mphepo ndi kuwinduka nayo.**

**Pakuti asayese munthu uyu kuti adzalandira kanthu kwa Ambuye; munthu wa mitima iwiri akhala wosinkhasinkha pa njira zace zonse. (Yakobo 1:6-8)**

Baibulo limati, “Zizindikiro izi zizawatsata onse okhulupirira.” Vesi imeneyi ikuyakhula za okhulupirira (Kachisi). Vesi imeneyi sikunena kuti “iye amene akukhulupirira,” kunena za munthu. Sichinali chikhulupiriro cha mmodzi kapena awiri olalikira chomwe chinabweretsa machiritso omwe analembedwa mu buku la Machitidwe. Chinali chikhulupiriro cha mpingo odzadzidwa ndi Mzimu.

Ngati Yesu sanachite zozizwa ku Nazaleni chifukwa chakusowa chikhulupiriro kwawo, kodi sichimodzimodzisoziso kunena kuti kusowa chikhulupiriro kwanthu kumatchinganso machiritso? Lero mpingo ukutsutsana kwambiri ndizomwe mpingo woyamba unachita popambana podalira pemphero. Sanavomerezebe maganizo a Baibulo pokhudzana matenda. Sanaphunzitsidwepo Mau a Mulungu zokhudzana machiritso. Koma amalozza dzala onse amene akulephera kulandira machiritso ndipo amalozza dzala onse amene akuyesetsa

kutumikira machiritso. Onse omwe amalalikira Uthenga Wabwino wamphumphu wachipulumutso ndi machiritso ndi mamasulidwe zinalephereka kuti zichitike ku “Nazaleti wosakhulupirira.”

### **KUSOWA CHIKHULUPIRO**

Kusakhulupirira ndi khalidwe lakuti Mulungu sangachite kapena sadzachita kena kalikonse. Kusakhala wosakhulupirira sikutathauza kuti uli ndichikhulupiriro. Mwachitsanzo, amene amati kulibe Mulungu. Okhulupirira ali ndi chikhulupiriro. Kusowa kusakhulupirira kwa anthu anzeru sikutathauza kuti ndekuti ali ndichikhulupiriro.

Pakuyenera kuti chikhulupiriro chamwa Mulungu chilowe mmalo mwa kusakhulupirira chifukwa ndi pemphero lachikhulupiriro lomwe limamudzutsa munthu wodwala (Yakobo 5:15). Mukuyenera kukhala ndi chikhulupiriro, kuyakhula mau achikhulupiriro, ndi kuchita mwachikhulupiriro. Mukuyenera kuyenda ndi chikhulupiriro osati zowoneka (kuyang’ana mmene nthupi liriri kapenaso zizindikiro zake).

Satana amayesetsa kuletsa machiritso pokupangitsani kuti muziyenda ndizowonka ndi maso mwala ndi chikhulupiriro. Amakupangitsani kuti muzikhala ndichidwi pa zizindikiro. Amakupangitsani kuti muziyang’ana kwa ena omwe amanena kuti achiritsidwa, koma sanachiritsidwe. Sichikhulupiriro chomwe chiri mwa inu kapena chikhulupiriro mu chikhulupiriro cha ena. Chikhulupiriro pachokha sichimachiritsa. Ndi Mulungu amene amachiritsa. Paulo anazindikira kuti olumala anali ndi chikhulupiriro chicmene chinampanga kuti achiritsidwe ndi Mulungu (Machitidwe 14:8-10)

Sizimatengera kukhala ndichikhulupiriro chachikulu kuti muchiritsidwe. Yesu anati chikhulupiriro changati mbeu ya mpiru chinali champhamvu kwambiri. Yesu amkakumana ndi anthu malingana ndi chikhulupiriro chawo. Pamene amkamva kuti akuyenera kupezeza ndi thupi lake, Amkapitako. Pamene anali ndi chikhulupiriro sikunali kofunika, Amkangoyakhula mau kuchokera patali ndipo machiritso amkachitika.

Pamene odwala sanmachiritsidwe, anthu nthawi zambiri amalozza dzala kusowa chikhulupiriro kukhala chifukwa. Koma pamene mukuphunzira phunziro lino, pali machitachita ena amene akuyenra kuti awaunikiridwe. Yesu sanaweruze anthu amene amkafuna machiritso chifukwa chopanda chikhulupiriro.

### **TCHIMO LA ENI LOSALAPIDWA**

Baibulo limatsimikiza ubale wachindunji omwe ulipo pakati pa tchimo la munthu ndi matenda nthawi zina:

**Cifukwa cace mubvomerezane wina ndi mnzace macimo anu, ndipo mupempherere wina kwa mnzace kuti muciritsidwe. Pemphero la munthu wolungama likhoza kwakukuru m'macitidweace. (Yakobo 5:16)**

Davide anati,” Ngati ndibisa zolakwa mu mtima mwanga, Ambuye sazandimva ine.”

Mulungu sanalonjeze kuwononga nthito za mdyerekezi mnthupi mwathu pamene tikukakamirabe ku ntchito za mdyerekezi mmoyo mwathu. Ngati muli chodetsa mu mtima mwa

munthu yemwe akudwala, akhoza wosachiritsidwa. Ngati muli machimo mu mtima mwa yemwe akutumikira, machiritso akhoza osachitika chifukwa Mulungu amakhala asakiumumva.

Mzimu osakhululuka kapena kusunga mangawa kumatchinga machiritso. Yesu anati, “Ngati simukhululikira anthu zolakwa zawo, ndekuti Atate wanu wakumwamba sangakukhululukireni zolakwa zanu.” Ngati Mulungu sangatikhululukire zolakwa zanthu pamene ife sitikukhululukira ena, sangatichiritse, chifukwa machiritso amakhudzaso kuyeretsewaso kwa moyo, mzimu ndi thupi.

### **KUKANA KUYERETSEDWA**

Yesu anafunsa munthu wolumala pathamanda la Betisayida:

#### **Ufuna kuciritsidwa kodi? (Yohane 5:6)**

Nthawi zambiri timangofuna machiritso kapena mamaslidwe okha. Mulungu akufuna kuthana ndi munthu yense ndikumuchiza thupi, moyo ndi mzimu. Chifukwa munthu ndi thupi, moyo, ndi mzimu, mfundo yawanthunthu ikuthauza kukhudza zonsezi. Sitingakhazikike pa machiritso akunthupi mkusiyapo moyo ndi mzimu, machiritso kupatulachipulumutso.

Mulungu ndi mzimu. Amalumikizana nanu kupyolera mu mzimu wanu. Mzimu wanu umatsogolera umoyo wanu wakuntupi. Moyo wanu onse umatsamira kwambiri pa uzimu wanu. Chifukwa inu ndi munthu amene muli wauzimu. Machiritso anthupi amayambira ku umzimu.

Pomwe Mulungu analenga munthu, mzimu wake unayenera kumatsogolera mphanvu za moyo wake pano pa dziko la pansi. Umayenera kukhala ndi ulamuliro pa maganizo ndi nthupi lake ndikulunganiztsa munthu yense momwe Mulungu akanakhalira. Pachiyambipo, mmunda wa Eden, munthu ali paubale wabwino ndi Mulungu.

Machiritso ndiopasa kungokhala opanda matenda. Ndi nthanzi la nthupi. Ndikubwereranso kukugwira ntchito kwa chiwalo chirichonse cha nthupi (nthupi, moyo, mzimu, kuphatikizapo maganizo, maimvaimva ndizina zotero)

### **KUSOWA KWA CHIGANIZO NDI ZOFUNA**

Yesu anafunsa munthu wopuwala pa thamanda la Betesda:

#### **“Ufuna kuchiritsidwa kodi?” (Yohane 5:6)**

Pamenepa munthu wolumalayo anayenera kupanga chiganizo. Anthu samafuna kuchiritsidwa. Amakodwera akamamveredwa chisoni ndi chidwi chimene amalandira chifukwa chakudwala kwawo. Ena amalandila chithandizo cha makhwala kupyolera pakupuma pantchito kapena kudzera malamulo ndipo samafuna kuti ataye zimezo. Ena amakhala ndi kufunitsitsa kuti apite kukakhala ndi Ambuye ndiye safuna kuchiritsidwa.

## **MABVUTO OKHUDZANA NDI KUPEMPHA KWANTHU**

Pali mabvuto ambiri okhudzana ndikupempha kwanthu kwa machiritso zomwe zikhoza kutchinga kuwonetseredwa kwake:

### **KUSAPEMPHA:**

Choyambirira cheni cheni, ndiponso chofunikira, nchakuti nthawi zina sitimapempha machiritso. Timapita ku makhwala kukafuna nthandizo kapena kwa abale kuti atitonthoze.

**Mulibe kanthu chifukwa simupempha... (Yakobo 4:2)**

### **KUSAPEMPHA MWACHINDUNJI:**

Nthawi zina, mapemphero amatchingidwa chifukwa samakhala achindunji:

**Mupempha koipa... (Yakobo 4:3)**

Ngati mukupepha molakwika, mapemphero anu ndekuti sanali achindunji. Simugwetse chandamale.

### **KUPEMPHA NDI CHOLINGA CHOLAKWIKWA:**

Nthawi zina timapemphera ndicholinga cholakwika:

**Mupempha ndipo simulandira, popeza mupempha koipa, kuti mukachimwaze pochita zikhumbitso zanu. (Yakobo 4:3)**

Anathu ena amafuna kuchiritsidwa, koma osafuna kuleka njira zawo zamachimo, zakudziko, ndi moyo ochita zoipa. Amafuna akhale bwino ndicholinga choti akapitirize kuchita zinthu zawonzo. Anthu akuyenera kulingalira funso iri: “Kodi cholinga nchani chofunira kuchiritsidwa? Kodi ndicholinga chofuna kubwerera kumoyo oipa omwe mmakhala? Kapena ndicholinga choti muzithamangathamanga kuchita ntchito zabwino malo okwaniritsa cholinga chomwe Mulungu alinacho painu?”

### **KUSAPIRIRA**

Nthawi zina sitipirira (Kupitirizabe) kupemphera kopitirizabe. Paulo yekha pachiyambi amkalalikira akudwala (Agalatiya 4:13-14) ndipo anachiritsidwa patsogolo pake. Pemphero silinagwire ntchito mwachanguchangu pa Epafrodito (Afilippi 2: 27) ndi Trofino amene anasiyidwa (2 Temoteo 4:20). Komabe pamapeto ake onsewa anachiritsidwa. (Dziwaniso kuti Paulo anapitiriza kupemphera chifukwa chakudwala kupatula kuti pa matenda awa panalibe machiritso ansanga).

Anth ena amaganiza kuti ngati ungapemphe machiritso kambirimbiri ndikusowa chikhulupiriro. Yesu sanaphunzitse kuti kukakamira pakupemphera kumawonetsa kusowa chikhulupiriro. Analimbikitsa zimenezi. Luka 11:1-13 amaphunzits akufunika kwa kukakamirabe m’mphephero mu fanizo la m’bale okakamira (vesi 5-8) za mkazi wamasiye ndi oweruza (Vesi 1-8). Danieli ndi chitsanzoso chomwe chimalimbikitsa kupirira. Mulungu

anamva pemphero lake poyamba pomwe, koma satana anatchinga mngero yemwe amkabweretsa yankho.

Musaleke ngati machiritso sanabwere panthawi yoyamba imene munapemphera. Kumbukirani kuti pali “kupempha, kufuna, ndikugogoda” milingo ya mapemphero. Nthawi zina umapempha ndipo yankho lapompopompo limabwera. Nthawi zina mukuyenera kufunafuna ndikupitiriza kugogoda musanalandire yankho kumapemphero ena. Mneneri Elisha anapemphera kuti moti otsike kumwamba. Nthawi ina anapemphera kasanu ndi kawiri kuti mvula ibwere.

Pitirizani kupirirabe mupemphero kufikira mutazindikira kuti pempho lanu lamveka. Pamene mwakhala ndi chitsimikizo chimenechi mu uzimu mwanu, kaneko yambani kumutamanda Mulungu ngakhale kuti yakho lowonoka ndimaso silinafike.

- Jehosafati ndi ana a Israeli anayamba kumulemekeza Mulungu mofuula asanayambe kuona yankho la mapemphero awo.
- Yesu anayamba kuthokozeratu Mulungu chifukwa chomuukitsa Lazalo.
- Pamene Abrahamu anali ndichitsimikizo cha mwana, sanapitirize kumangopemphera. Anamkulupirira ndikuyamba kumukweza Mulungu.

### **KUSAMVERA NDONDOMEKO YAMACHIRITSO**

Nthawi zina Mulungu amapereka malangizo apaderadera mundondomeko yamachiritso. Mwachitsanzo, kupyolera mwa mneneri Elisa, Mulungu anamuza Namani kuti apite kukasamba mu mtsinje wamatope kuti alandire machiritso (2 Mafumu 5:1-14). Nthawi zina kumvera kophweka ndikomwe kuli pakati pa inu ndi chozizwa chanu.

### **KUZINDIKIRA THUPI LA KRISTU MULAKWIKWA**

Werengani 1 Akorinto 11:27-30. Kutu mukhale ndichithuzithuzi chabwino muwerengenso Luka 22:2-20, Mateyu 26:27-29, ndi Marko 14:22-25. Kufoka ndi kudwala ndizotsatira chifukwa sitilandila thupi la Kristu moyenera. “Kuzindikira: ndiko kuphunzira ndi kumvetetsa chithu pochiyesa, kufufuza, ndi kuchizindikira bwino.

Tikhoza kulephera kuzindikira Thupi la Kristu mu njira zitatu:

### **TANTHAUZO LA MWANZI NDI THUPI:**

Timalephera kuzindikira pamene sitikumvetsa tanthauzo la chipatso champesa ndi mkate zomwe ndi zifanifani za mwanzi ndi thupi Lake. Izi ndizomwe zinachitika pamene Yesu anaphunzitsa chiphunzitso chimenechi pa Yohane 6:66 ndipo ambiri anabwerera kumutsatira Iye. Sanamvetsetse tanthauzo la uzimu pazomwe amkaphunzitsa. Pamene ambiri akuzindikira mwanzi ochotsa machimo, kawirikawiri samazindikira tanthauzo lake leni leni la jthupi. Thupi linali lobweretsa machiritso, ndetikhoha kulidya ndipo titha kuchiritsidwa. (Onani Yohane 6:48-58 ndi Luka 6:48-51).

### **KUGAWANIKANA M'THUPI:**

Nthawi zina timalephera kuwazinfikira abale ndi alongo amene ali mbali imidzi ya thupi la Kristu ndipo kugawanikana kumakhachitika m'mkachisi. Timadya ndikumwa mosayenera ngati sititimazindikira ubale wanthu ndi abale ndi alongo mwa Ambuye. Paulo anafotokoza pa 1 Akorinto 3:1-13 kuti akhrisitu ozikonda sangadye nyama (thupi) la Atate chifukwa chakuzikonda kwawo.

### **KUDYA MOSAYENERA:**

Timadya mosayenera pamene tikudya mgonero ndi moyo osaziyesa. Kufoka ndi kudwala ndizotsatira zake. Ichi nchifukwa chake Paulo ananena kuti kuziyensa nokha mwauzimu ndikulapa tisanadye mgonero.

### **MZIMU WOYIPA SUNATULITSIDWE**

Ena samalandira machiritso chifukwa mtenda yawo ndi ntchito ya mzimu woyipa umene ukuyenera kutulitsidwa. Amafuna pemphero lolimba kuposa lamachiritso. Mu nyengo zimene zinabweretsedwa ndi mzimu woyipa, Baibulo linalamba kuti mdani anatulutsidwa kuti machiritso achitike.

### **KUSOKONEZA MALAMULO ACHILENGEDWE**

Mulungu yemweyo anati “Ine ndine Mulungu amene nakulichiritsa” anaperekanso malamulo aumoyo ndi ukhondo kwa anthu Ake. Anthu ena samalandira machiritso chifukwa amasokoneza amalammulo achilengedwewa. Mwachitsanzo, munthu kumapitiriza kumwa mowa nde mkumadabwa kutnchifukwa chani machiritso okhudza ndi thenda yachiwindi sakuchitika. Akhoza kumapitiriza kusata fodya mkumadabwa kuti nchifukwa chani matenda a khansa ya mapapo sakuchitika.

### **NTHAWI YOYIKIKA YAKUFA**

Baibulo limaphunzitsa kuti pali nthawi yoyikika yakufa (Mlaliki 3:4 ndi Ahebri 9:27). Ngakhale mneneri wamphamvu Elisa, amene anachita zozizwa zamachiritso ndikumasa, ” anadwala matnda amene anamutengera ku imfa” (2 Mafumu 13:14). Muphunzira mmene mungathanirane ndi zotchinga zimenezi pamene muzaphunzire mmene mungatumikirire kumatenda akulu monga ngati mbali imodzi yamalangizo a momwe mungatumikirire machiritso mu chaputala 8.

### **KUKUMBUTSA KOMALIZA**

Tinatsekula phunziro lino ndimafunso ambiri:

Ndimachitachita ati omwe amasokoneza machiritso? Nchifukwa chani anth ambiri sachiritsidwa? Nchifukwa chani ena amachiritsidwa pamena ene ayi? Nchifukwa chani achikunja ndi ena owoneka ngati akhrisitu amachiritsidwa pomwe anthu achilungamo ndiozipereka sanalandirebe machiritso?

Machitachita omwe mwaphunzira mu phunziro lino ndizochitika zina zomwe zingathe kusokoneza machiritso ndimamasulidwe. Nthawi zonse kumbukirani kuti...

**Zinsinsi nza Yehova Mulungu wathu; koma zobvumbuluka nza ife ndi ana athu kosatha, kuti ticite mau onse a cilamulo ici. (Deuteronomo 29:29)**

Chikhulupiriro chimafunikira: Chikhulupiriro. Ngati muli ndimayankho onse, simungamufune Mulungu ndi chikhulupiriro. Mulungu yekha amafunsa kuti muchite mwachikhulupiriro pa Mau Ake, osati kupereka mayankho.

Pomaliza, nayo mfundo yokhudzana ndi machitachita amachiritso. Inapangidwa ndi mtumiki wotchuka yemwe anatumikira kwa zaka zambiri pa machiritso ndi mamasuridwe:

*“Ine ndekha, zalalikira Uthenge Wabwino onse ngati zawone munthu wosapulumsidwa kapena kuchiritsidwa ngati ndiri ndi moyo. Ndakozeka kukhazikitsa chiphunzitsa changu pa Mau a Mulungu osasitha, osati zochitikachitika.”* -F.F. Bosworth

## MAYESO OZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera.

---

---

---

2. Perekani tanthauzo la mau oti “zochitika.”

---

---

---

3. Fotokozani ina yamiyambo ya munthu yomwe imasokoneza machiritso.

---

---

---

---

4. Fotokozana machitachita ena omwe amasokoneza machiritso.

---

---

---

---

---

---

---

---

---

---

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)



## ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Pamene mukupephera pemphero limene linaperekedwa ndi Yesu (Limadziwikaso kuti “Pemphero la Ambuye”), limaphatikizaposo kupempherera machiritso.

**“Atate anthu muli Kumwamba”:** Pomwe mukupempha kwa Atate anthu, makhala mukupempha kudzera pa dzina Lake, kuphatikizapo kuti “Atate ndinu ochiritisa.”

**“Ufumu wanu udze, kufuna kwanu kuchitidwe monga kumwamba chomwechonso panso pano”:** Kulibe matenda kapena tchimo kumwamba. Tikuyenera kuchita chifuniro cha Mulungu panso pano mongaso mmene ziriri kumwamba, kuti tilimbane ndi matenda ngakhalenso tchimo.

**“Mutipatse ife chakudya chathu chalero”:** Yesu anati mkate ndiwa ana (okhulupirira). Machiritso akuthupi ndi mbali imodzi wamkate wa ana (Mateyu 15:21-28).

**“Mutikhululukire ife zochimwa zanthu monga ifenso tiwakhulukira adani anthu”:** Ndime imeneyi imakamba zamachiritso auzimu.

**“Musatengere ife kokatiyesa, koma mutipulumutse ife kwa oipawo”:** Matenda akuyenera kukanizidwa monga mmene mungakanizire mayesero.

2. Mwaphunzira kuti Mulungu sigwero lamazunzo koma akhoza kugwiritsa ntchito pofuna kukwaniritsa zolinga zake. Onani zitsanzo zotsatiranzo zomwe zikukamba zazimenezi:

- Miriri ya A Igupto	Eksodo 7-11
- Khate pa Miriam	Numeri 12:10
- Kudwala kwa mfumu Yoram	2 Mbiri 21:18
- Khate la Gehazi	2 Mafumu 5:27
- Imfa ya mwana wa Davide	2 Samueli 12:18
- Imfa ya ana a Eli	1 Samueli 2:34
- Kuzuzika kwa Yobu	Buku la Yobu
- Kugulitsidwa kwa Yosefe	Genesis 45:5-7
- Kupachikidwa kwa Yesu	Marko 14:35-36 ndi Aroma 5:6-12
- Kuponyedwa ndende kwa Paulo	Afilipi 1:12,19
- Minga munthu la Paulo	2 Akorinto 12:7

3. Phunzira zambiri zomwe Baibulo limakamba zokhudzana ndi umphumphu:
  - Pomwe anthu amangofuna machiritso okha, Yesu amafuna kuthana ndi munthu yense wathuthu. Anati kwa munthu wolumala pa Betesda, “Ufuna kuchiritidwa kodi?” (Yohane 5:6)

- Yesu anabwera kuzatumikira kwa onse amene sanali amphumphu-osweka mtima, odwala, oponderezedwa. Agwiro safuna sing'anga: Mateyu 9:12; Marko 2:17; Luka 5:13
- Yesu anali gwero la ugwiro: Machitidwe 9:34; Yohane 5:15
- Onse amene anamukhudza Yesu anachiritsidwa: Mateyu 9:21-22; 14:36; Marko 5:28-34
- Yesu anamuchiritsa wantchito amene anamkadwala: Luka: 7:10
- Anachiritsa wolumala: Yohane 5:9
- Ophunzira, kupyolera mumphamvu ya Mulungu, anamuchiritsa wolumala: Yohane 5:9
- Anachiritsa manja onse: Mateyu 12:13; Marko 3:5; Luka 6:10

## CHAPUTALA 18

### “PAMENE MUKUMUKA, KACHIZENI”

ZOLINGA:

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba Vesi yotsogolera osawonera.
- Kufotokoza zokozekera zoyamba za utumiki wamachiritso.
- Kulemba mwachidule ndondomeko zamomwe machiritso angatumikidwire.
- Kufotokoza mmene tingawatsatirire mkuwasamala onse omwe achiritsidwa.
- Kufotokoza mmene tingawatsatirire mkuwasamala onse omwe sanachiritsidwe.

**VESI YOTSOGOLERA:**

**Ndipo pamene mulikumuka lalikirani Ufumu wa kumwamba wayandikira**

**Chiritsani akudwala, ukitsani akufa, konzani akhate, turutsani ziwanda: munalandira kwa ulere, patsani kwaulere. (Mateyu 10:7-8)**

### CHIYAMBI

Mwaphunzira kuti machiritso ndi mamamasuridwe ndi machitachita a Ufumu wa Mulungu. Mu phunziri lino muphunzira mmene mungatumikirire machiritso. Muphunziro lotsatira muzaphunzira mmene mungatumikirire mamasuridwe.

### ZOKOZEKERA ZOYAMBA

Chikhulupiriro chimadza pakumva Mau a Mulungu okhudzana machiritso. Kuti mukulitse chikhulupirio chanu, mukuyenera kuphunzira china chirichonse chamachiritso chomwe chiri m’Baibulo. Werengani Chipangano Chatsopano ndi maganizidwe atsopano. China chirichonse chimene Yesu anawauza omutsatila kuti achite, inuso mukuyenera kuchita zimenzo. Zonse zimene anati achita, yembekezeni kuti achita.

### ZIKOZEKERETSENI NOKHA:

Ngati anati mukhoza kuchiza odwala kupyolera mu mphamvu yake, ndeyembekezerani kuona iwo akuchizidwa. Ngati anati muzatulutsa ziwanda, nde chitani izi kupyolera mu dzina Lake ndipokhulupirirani kuti zikumverani. Kanani ziphunzitsa zonse za munthu zomwe munalandira. Khulupirirani kuti Chipangano Chatsopano chimachita zonse zomwe chimanena. Chimvomerani kuti ndichoona ndipo chitani moyenerera. Ndinu kazembe wa Keistu (2 Akorinto 5:20). Kazembe samakaika kuti dziko lomwe akuliimirira liikira kumbuyo mau ake.

Salani kudya ndi kupemphera musanayambe kutumikira. Onani chitsanzo cha Paulo pa Machitidwe 28:8. Popeza mphamvu ndi ulamuliro ochiritsa umachokera kwa Mulungu, ndendikofunika kuti pakhale kulumikizana kwambwino. Kuzuzidwa kwina ndi ziwanda kuzachiritsidwa paakupemphera ndikusala kudya. Yesaya 58 imaphunzitsa kuti Mulungu amalemekeza kusala kudya komwe kumaika chidwi pazofuna za ena.

Yambani kutumikira kwa odwala ngakhake kuti simukumvetsetsa chinachirichonse zokhudzana ndi machiritso akumwamba, monga ngati momwe munayambira kuchitira umboni pomwe munapulumsidwa ngakhale kuti mumkhayenera kuphunizra kaye zokhudzana ndi moyo wa Chikristu. Yambani kutumikira kuyambira pazomwe madziwa zokhudzana ndi machiritso. Pomwe mukuyenda mukuwala komwe mwapatsidwa, muzalandira kuwala kwambiri. Tengani maganizo oti kulibe nyengo yopanda chiyembekezo. Pali anthu omwe akhala opamba chiyembekeze za izo.

### **ZOKOZEKERA ZOYAMBA KWA ENA:**

Ngati malimbikitsa odwala kuti apephereredwe popanda malangizo oyerenerera, zilingati kumulimbikitsa munthu wosapulumsuka kuti alandire Yesu kukhala mphulumutsi wake popanda kudziwa kuti Ndindani, akuyenera kuzindikira machimo awo, ndikufunikwa kwachipulumutso chawo.

Nthawi zina, Mulungu amachiritisa popanda malangizo oterewo. Koma kumbukirani: Potumikira machiritso, mukuyenera kugwiritsa bwino ntchito njira zonse zimene mau a Mulungu anapereka kuti muwone mmene ntchito itachitikire. Chikhulupiriro ndi njira imodzi imene mphanvu ya machiritso a Mulungu imabwerera ndipo imabwera ndi mau amachiritso. Nde malangizo ndi ofunika. Yesu anasakaniza kulalikirira ndi kuphunzitsa ndi machiritso ndipo analamula Omutsatira Ake kuchachitaso chimodzimodzi.

Anthu akuyenera kudziwa chimene mau a Mulungu amanena kwa komwe kumachokera machiritso, gwero ndi choyambitsa chamatenda, malonjezano amachiritso, ndi ndondomeko za Baibulo zolandirira machiritso ndimmene tingakhali anthanzi.

Pandondomeko yopereka machiritso kwa okhulupirira, kusala kudya ndi kupephera kwa odwala kukhoza kukhala kothandiza. Izi sizofunika kuti machiritso abwere, koma kumbukirani: tikuyenera kugwiritsa ntchito njira ina iriyonse yopezeka m'Baibulo. Mulungu anatsimikiza zakupempha kwanthu ndipo Yesaya 58:6-8 imatsimikiza za kufunika kwa kusala kudya ndi kupemphera pokhudzana ndi umoyo wabwino.

### **NTHAWI YAUTUMIKI**

Nawo malingaliro azomwe ziyenera kuchitika pa nthawi yotumikira machiritso. Kumbukirani izi ndi ndondomeko chabe. Mukuyenera kumvomera chitsogonzo chosiyanasiyana chochokera kwa Mzimu Woyera. Ena mwamalingalirowa amangogwira ntchito kwa anthu ochopa akutumikiridwa, pamene ena amagwira ntchito potumikira ku gulu la anthu:

### **KUPANGA MALO ACHIKHULUPIRO:**

Pangani malo achikhulupiriro. Munayamba kale kuchita zimenezi pomwe matumikira Mau pa machiritso, koma mukufunikaso kutenga mkwerero lina popanga malo achikhulupiriro. Azungulireni odwala ndi anthu achikhulupiriro ndi otsimikizika mtima. Lolani kuti amve maumboni a anthu onse amene anachiritidwapo. Kumbukirani kuti kusowa chikhulupiriro kumatchinga ngakhale utumiki wa Yesu ku Nazarete.

Machiritso akhoza kubwera kupyolera pakulambira ndi kutamanda ngakhale popanda pemphero lamachiritso chifukwa Mulungu amakhala matamando a anthu ake. Pamene tikulambira Mulungu, amapezeka kuti achiritse. Kuwasendeza anthu pa mulingo pachiganizo

chamachiritso awo, monga mmene mungachirite ndichipulumutso. Kumbukirani momwe Yesu amanamfusira munthu wolumala, “Kodi ufuna kuchiritsidwa?” (Yohane 5:6).

Mufunzeni munthu kuti awonetse chikhumbokhumbo chawo chamachiritso. Pa gulu mukhonza kuwafunsa iwo kuti ayime, abwere kutsogolo, aimike manja awo, kapena kuika dzanja lawo pamalo pomwe akudwalapo pa nthupi pawo. Izi zimathandiza kuti awonetse chikhumbokhumbo chawo chofuna kuchiritsidwa. Ndi kuchita kwachikhulupiriro kwa iwo, komaso izi zimakuthandizani kuzindikira onwe akufuna kutumikiridwa.

### **PEMPHERERANI CHIDZIWITSO:**

Pemphererani nzeru ndi chidziwitso musanatumikire machiritso. Gawani nzeru ya kumwamba yomwe Wakupatsani. Mulungu anthu kukuwululirani:

**Mau a chizindikiro:** Mau a chidziwitso amaulula chindunji cheni cheni cha munthu kapena mmene alili nde muzazindikira momwe mungapempherere. Mau achizindikiro akhoza kumphatikizapo kuzindikira mozama, kutsikizika mu uzimu, maganizo, mau kapena maimvaimva. Mau a chidziwitso amatha kuvumbulutsa kuti matendawo ndi otani kapenanso kuti nchifukwa chani kuti munthu akudwala chonchi.

**Vesi ya Mmau:** Mulungu akhoza kukupatsani “Rhema” (apaderadera) Mau a Mulungu chifukwa cha nyengo imeneyo, matenda, munthu kapena gulupu.

**Masomphenya:** ichi ndi chinthunzinthunzi cha mmaso amalingaliro chokhudzana ndi omwe mukawatumikire.

**Mau a chikhulupiriro:** Awa ndi mau apaderadera achirimikitso ndi chikhulupiriro makamaka kwa munthu ameneyo.

**Kudzodza kwapaderadera:** Kudzadzidwa ndi mphamvu mwadzidzi, umayamba kumva kutentha kapena umakhala ndikulimbika mtima kwambiri. Nthawi zina kudzodza kumeneku kumabwera, umayamba kuyenda nako. Koma musadikire kudzodz kwapaderaderaku kuti mupempherere odwala. Mukuyenera kutsata malangizo a Yesu kaya mukufuna kapena ayi.

**Kuchita mwachikhulupiriro mwapaderadera:** Nthawi zina Mulungu azakutsogolerani kukamuza munthu kuti achite zina mwachikhulupiriro zomwe zinabweretse machiritso.

### **KUZINDIKIRA MVUTO:**

Gwiritsani ntchito uthenga pochokera pakufusa mafuso ndi nzeru zomwe Mulungu wakupatsani kuti muzindikire ngati mvutoliri:

**Lakuuzimu:** Awa ndi mamvuto omwe amakhudzana ndi tchimo ndipo amafunika kutumikiridwa ndi machiritso auzimo (chipulumutso, kulapa ndi kukhululidwa kwa tchimo).

Ngati Pali gwirizano pakati pa tchimo ndi nthenda (ndipo tawona kuti palidi gwirizano), ndekuti paligwirizano pakati pa kukhululukiridwa ndi kuchiritsidwa, ndi ntchito ya Mzimu Woyera kubvumbulutsa popeza mwantchito Yake imodzi ndi kutsutsa ndi kukuza.

Musamachite machawi polumikiza matenda ndi tchimo. Kumbukirani kuti matenda onse mwaphunzira kuti simatenda onse omwe ali zotsatira za tchimo la mwini. Ngati pali tchimo,

nde ndi udindo wa Mzimu Woyera kubvumbulutsa popeza cholinga Chake ndi kutsutsa ndi kukoza.

**Zakunthupi:** Awa ndi matenda akunthupi, kumvulala, kapena madwale. Pemphererani machiritso akunthupi.

**Maimvaimva:** Awa ndi mabvuto monga kudera nkhawa, khwiyo, kuwawidwa mtima, kukhumudwa, kulephera, kukhala ndi chikaiko, kaduka, kuzikonda, kusokonekera, kusakhululuka, ndi zotsatira zamabvuto akale. Anthu awa akufunika machiritso amaimvaimva. Machiritso amenewa amatchulidwa kuti “machiritso amkati,” koma liwu lagwiritsidwa ntchito udyo ndi anthu ena. Sikofunika kupitaso pambuyo mkukayeserera zonse zomwe zinachitikazo. Sikofunika kuti pachite kutenga masabata, miyezi kapenaso zaka kuti uchire kumabvuto amenewa. Ngati mungachite zimenezi, ndekuti mukuyesera kuchiza munthu wakale mmalo momuthandiza kuti akhale olengedwa mwatsopano mwa Kristu.

Mabvuto amaimvaimva kawirikawiri amakhudzana ndi mmene munthu akukhalira. Amatha kusokoneza mabanja komaso ubale wa munthu. Machiritso amabwera kupyolera pakuzindikira mvuto, kupempha chikhululukiro, ndikhuwakhululukira onse omwe anatengapo gawo pobweretsa mabvutowo.

Chotchinga chachikulu cha machiritso amaimvaimva kawirikawiri chaimakhala kusakhululuka, nde machiritso amaimvaimva ndikuphatikizapo kuchiza maubwezi. Tinayitanidwa kukhala atumiki oyanjanitsa (2 Akorinto 5:18-21). Anthu akuyenera kuyanjanitsidwanso ndi Mulungu ndi munthu, ndipo apa ndipamene maimvaimva, maganizo ndi machiritso amkati amabwera.

Mukhoza kufuna kumuphunzitsa munthu zokhuzana ndi kukhululuka. Kukhululuka si:

- Kulungamitsa zolakwa zawina zomwe akuchitirani. (Mwachitsanzo, kunena kuti, ” pochita zimenezi anali atapanikizika.”)
- Sikukana kuti pachiyambi munamvulazidwa.
- Kukana zomwe zinachitidwa kwa inu.
- Kudikira nthawi yochiritsidwa pakumvulazidwa. (Sichoncho).

Kukhululuka kweni kweni kumabwera ndi:

- Kumvomereza kuti zomwe zinachitika kwa inu zinali zolakwika, ndizochita za anthu ochimwa mudziko la uchimo. Sikufunika kubwereraso pambuyo kumakakumbukiranso zomwe zinachitikazo, koma mmalo mwake mukhoza kuthana nazo pozikana. Mvomerezani zomwe zinachitikazi ndi momwe zinakhudzirani.
- Perekani kumvulazidwa kwanu kwa Mulungu ndipo Mumupemphe kuti akuchiritseni kumaimvaimva oipa. Simungaiwaliretu choonadi cheni cheni cha

zomwe zinachitika ndi mmene zinakukhudzilani koma chomwe mukufunika ndi machiritso pa zoipa pa zomwe zinakuchitikirani.

- Kumphepha Mulungu kuti akuthandizeni kukhululukira ena omwe anatengapo mbali, nde akhululukireni iwo monga momwe Kristu amakukhululukirani inu. Zindikirani kuti Mulungu akukhululukirani pamene inu mukukhululukiranso ena: “Mutikhululukire ife zolakwa zanthu monga ifenso tikhululukira amangawa anthu.” Munthu akuyeneranso kuzikhululukira yekha (kumva kulakwa pazolakwa zimene wachita) ndipo akuyenera kupempherera machiritso pa maimvaimva ake. Nazo ndondomeko za momwe munthu angazikhululukire yekha:
  - Mvomerezani tchimo lomwe likukupangitsani kulakwa ndi maimvaimva auchimo, mvomerezani kwa Mulungu, ndipo lapani. Mpempheni kuti akukhululukireni machimo anu ndipo achiritse maimvaimva anu.
  - Zindikirani kuti Mulungu akakhululukira, amaiwala (amawaponya kutali machimo anthu monga mmene kuliriri kutalikana kwa kummawa ndi kumadzulo).
  - Funsani 1 Yohane 1:8-9 ndi Aroma 8:1

**Zamubongo:** Awa ndimabvuto amene amachokera pakuganiza molakwikwa, chiwembu cha satana maganizo, kusaganiza mokwanira, ndizita zotero. Pemphererani machiritso.

**Ziwanda:** Izi ndi nyengo zobwera chifukwa cha machitachita aziwanda monga kugwidwa ndi chiwanda. Muphunzira mmene mungathanirane ndi zimenezi muphunziro lotsatira potumikira mamasuridwe. Nthawi zonse kumbukirani kuti mabvuto amiyamba amakhudza munthu yense. Pamene mukutumikira, chitani ndi munthu yense monga mmene Yesu anachitira, osangoti matenda okha. Munthu ndi nthupi, moyo, ndi mzimu. Uthuthu ukutathauza kuchitanazo zonsenzi.

### **PEMPHERANI PEMPHERO LAMACHIRITSO:**

Mutantha kuwona mmene ziririr, mukuyenera kupemphera pemphero lamachiritso. Koma nthawi zina, musamadabwe ngati Mulungu atakuzani kuti musapemphere kapena muchedwe kupemphera. Mwachitsanzo, kupyolera pofunsa mafunso mukhoza kuzindikira kuti munthu sakufuna machiritso chifukwa aluza cholowa chaulumali wawo (Izi zinachitika mu mkumano wina wamachiritso).

Ambuye akhoza kukuuzani kuti muchedwelepo popempherera machiritso akunthupi kufira atazakuuzaniso kapena kuti munthuyo athane kaye ndi mvuto la tchimo. Pamene mukupemphera, muzipephera pemphero lachikulupiriro lomwe limalunjika pamvuto lenileniro. Kumbukirani kuti simukuyenera kumukakamiza Mulungu kuti achiritse pakudzera kutalika ndi kukuwa kwa kupemphera kwanu. Monga kuti chipulumutso chiripo kale, izinsu ziri chimodzi modzi ndi machiritso. Monga momwe kuti chipulutso chimabwera ndi chikhulupiriro, ndeziriso choncho ndi machiritso. Mulungu akufuna kuchiritisa, chimodzimodzi monga amafuna kupulumutsa.

Chifungulo cha kuyakhidwa kwa pemphero ndi kupemphero malingana ndi chifuniro cha Mulungu “Ngati ndichifuniro cha Mulungu.” Yesu sanapemphere “Chiritsani ngati chiri chifuniro Chanu.” Pempherani pemphero lakuti kufuna kwa Mulungu kuchitidwe “kufuna kuchitike monga chomwecho Kumwamba” kapena “maringana ndi chifuniro Chanu.” Uku mkuzindikira ukulu wa Mulungu.

Ngati mkotheke, ngwiritsani ntchito okhulupirira ena kuti atumikire nanu limodzi. Pamakhala kuchulukitsa kwa mphamvu ya uzimu pamene anthu ochuluka akupemphera (Onani Mateyu 18:19). Utumiki wakunthupi sumalimbikitsa anthu omwe akupambana mu mphatso za machiritso ndi onse omwe alandira machiritso mkuyamba kupereka ulemu kwa iwo eni kapena kwa munthu wina. Wina aliyense wamu nthupi la Khristu alinayo mphatso imodzi ya uzimu. Utumiki wopambana ndi pomwe...

**monga yense walandira mphatso, mutumikirane nayo, ngati adindo okoma a cisomo ca mitundu mitundu ca Mulungu. (1 Petro 4:10)**

Pemphero lanu lamachiritso likhoza kukhala limodzi mwa awa:

- Zopempherera Marko 7:32-35
- Kulamula Luka 4:38-39; Marko 7:32-35; Yohane 5:8; Machitidwe 3:6; 9:40
- Kupembedzera Machitidwe 32
- Kudzudzula ndi kutulutsa Marko 9:25

Mapemphero anau amakhudzanaso ndi malangizo kuti mukachite zinthu zina mwapaderadera, monga momwe Mulungu akufunira (Onani Yohane 9:1-7). Musamawakakamize anthu kuti aleke kumwa makhwala. Mulekeni Mulungu kuti awatsogolere Yekha kuzimenezi. Nthawi zonse pempherani mudzina la Yesu. Kumbukiraniso kuti sikusowa chikhulupiriro kupemphera kambirimbiri. (Kumbukirani zomwe Yesu anaphunzitsa zokhudzana pakupirira popemphera.)

**KUMULEMEKEZA MULUNGU CHIFUKWA CHA MAYANKHO:**

Pemphero lanu lizitsatana ndi matamando kwa Mulungu chifukwa chamachiritso. Kumbukirani kuti anthu nkhumu akhate omwe Yesu anawatumikira, onse anachiritsidwa koma mmodzi yekha ndamene anabwerera kukamutamanda chifukwa chamachiritso ake. Mulungu alemekedwe ndi chikhulupiriro osati ndi maso chabe. Mwachita zomwe mau a Mulungu amakuzani kuti muchite.

Khulupirirani kuti Mulungu wachita zimene ananena kuti achita. Muthokozeni chifukwa chazimenezi. Yesu anamuthokoza Mulungu chifukwa chamachiritso pemphero lomwe anapemphera Lazaro asanatuluke mmanda.

**UTUMIKI OLONDOLA**

Ndikofunika kwambiri kuti onse amene achiritsidwa akuyenera kulandira utumika olondoledwa. Yesu anapereka malanginzo oti tizilondola onse amene alandira machiritso ndi mamasulidwe.

Anayakhula ndi munthu amene anachizidwa ku khate:



**Ndipo iye anamuuzitsa, kuti asanene kwa munthu ali yense; koma ucoke, nudzionetse wekha kwa wansembe, nupereke nsembe ya pa cikonzedwe cako, monga adalamulira Mose, kukhale umboni kwa iwo. (Luka 5:14)**

Anamuza mzimayi wochimwa amane anachiritsidwa:

**Pita kunyumba kwako, nufotokozere zazikuruzo anakucitira iwe Mulungu... (Luka 8:39)**

Kwa mzimayi amene anagwidwa akuchita chigololo anati:

**... Inenso sindikutsutsa iwe; pita; kuyambira tsopano usacimwenso. (Yohane 8:11)**

Ngati mukutumikira nokha kwa munthu, mukuyenera kukhala ndi nthawi yomulondola nokha. Ngati pa msokhano waukulu, mukuyenera kupereka ulangizi mukamaliza kutumikira, kapena mamawa wake. Ngati mukutumikira pa mpingo, afunsemi abusa kuti azilondola onse amene achilitsidwa.

Malangizo olondola akuyenera kukhudza zinthu izi:

- Tingatani kuti tikhalebe ochiritsidwa.
- Tichite chani ngati sanachiritsidwe.

### **TINGATANI KUTI TIKHALABE OCHIRITSIDWA:**

Mphunzitsani onse omwe angochiritsidwa kuti:

#### **Azindikire kuti ndi chiwembu cha satana:**

Monga momwe satana amayesera amane wangopulumutsidwa kumene, amayesaso munthu wina aliyense amane wachiritsidwa. Monga momwe mungalepherere chipambano cha uzimu, mothanso kulephera chimodzimidzi kuthupi. China chirichonse chomwe makhulupirira Mulungu muuzimu mwanu, muzayensedwa kumbali imeneyo. Satana azakuyensani inu pa:

- Zizindikiro: Machiritso nthawi zina amachitika pang'onopang'ono. Zizinfikiro zanu mwina sizingachoke mwachangu. Zizizindikiro zanu mwina zikhoza kuipirabe. Mukhoza kumatetha nthupi, koma iyi ikhoza kukhala njira imene nthupi likulimbana ndi matenda monga ngati mbali imodzi ya machiritso. Muziyenda ndi chidziwitso cha uzimu, osati ndi zowoneka ndi maso. Musamke kuzungulira kumalengeza za zizindikiro zanu, kwinaku musamanane pa zimenezo. Ngati mwafunsidwa muziyakha kuti “inde, ndiridi ndi zizindikiro za \_\_\_\_\_, koma ndi mikwingwirima Yake ndachiritsidwa.” Muzika chidwi chanu pa zinthu zosawoneka mwalo mwa zizindikiro. Zizindikiro zikhoza kukuchotsani pa Mau a Mulungu, pa maso Pake, malonjezano Ake, ndi mphamvu Yake. Musamayakhule mau olakwikwa omwe amakweza chiwembu cha satana panthupi panu. Amena amakulibikitsani inu kwambiri-kusowa kwazizindikiro kapena Mau a Mulungu amene amanena kuti Iye ndi mchiritso wanu? Chidwi chanu ndi chani?

- Kukupangitsani inu kuti muziyang'ana kwa ena: Kuloza kwa ena omwe amaganiza kuti anachiritsidwa, koma pano akudwalaso. Musamayang'ane kwa omwe amanena kuti anapulumsidwa koma tsopano akukhala mu uchimo ndipo akugwiritsidwa ntchito ngati chitsanzo pokana chowonadi chachipulumutso?
- Matha: Kuwopa kuti matenda anu atha kubwereranso.
- Anthu olakwika omwe akuzungulilani: Onse amene adzadzidwa ndi kusakhulupirira omwe amadzala ambeu yachikaiko mwa inu.

### **Kanizani ziwembu za satana:**

Muzikhalabe pamalo achikhulupiriro popitiriza kuwerengnga Mau a Mulungu amachiritso. Mulemekezeni Mulungu chifukwa chamachiritso anu. Muzilumikizanabe ndi mchiritso wanu popemphera. Chitirani umboni machiritso anu kwa ena, kupereka matando kwa Mulungu. Njira imodzi yomugonjetsera satana ndikupyolera mau a umboni wanu. Kanizani ziwembu zasatana ndi “Rhema” Mau a Mulungu potenga veis yapaderadera yokhudzana machiritso. Musamagwedezeka mchikhulupiriro chanu, munthu yemwe amangogwedezeka sazalandira kuchokera kwa Mulungu (Yakobo 1:6-8). Limbikani (Limbanani) mwachindinji mchikhulupiriro pamachiritso anu (Aroma 10:9)

Makana ziwembu za satana pamene mukugwiritsa ntchito ulamuliro wanu wauzimu omwe mkuphatikizapo:

- Mau a Mulungu.
- Mwazi wa Yesu.
- Mau a umboni wanu.
- Ulamuliro womanga kapena kumasula.
- Pemphero ndi matendo.
- Zida zakhondo zomwe ziri pa Aefeso 6:10-18.
- Ulamuliro ndi mphamvu ya Mzimu Woyera.

(Ngati simunabatizidwe ndi ubatizo wa Mzimu Woyera mukuyera kuusakasaka. Mzimu Woyera amaperaka mphamvu yomwe imakuthandizani kuti musungebe machiritso anu. Monga mmene mutaphunzirire mu chaputala chotsatira, izi ndi zofunika makamaka pa mamasuridwe kumachitachita aziwanda.)

### **Sithani kakhaliidwe kanu:**

Kubwereranso kumoyo wochimwa kukhoza kutanthauza kuti kubwereraso kwa matenda (Yohane 8:11). Yendani mkumvera kwa Mulungu ndi Mau Ake. Kuchimwa kwadala kukhoza kutayitsa machiritso (Yohane 5:14). Kubwereranso ku machitachita opanda pake kukhoza kuchititsaso kuti mtenda ibwerereso. Machitachita opanda pake ndi tchimo leni leni, lomwe limadetsa kachisi wa Mulungu.

### **Tsatirani ndondomeko za Baibulo za kukhala moyo wa nthazi ndi machiritso:**

Baibulo limaperaka ndondomeko zokhalalira moyo wathanzi. Pezani phunziro la Harvestime lotchulidwa kuti “Nkhon do ya nthupi” kuti muphunzire ndondomeko zimenezi mwatsatanetsatane.

### **Bwererani kuchipatala kuti akatsimikize kuti mwachiradi:**

Ngati mwakhala kuti munali pamakhwala, bwererani kwa dotolo wanu kuti akatsimikize kuti mwachiritsidwadi. Pansi pa Chipangano Chakale, amsemble anali ngati madotolo. Amayeza matenda ndipo amkalengeza machiritso. Yesu anamuza wakhate yemwe anamuchiritsa:

**...koma ucoke, nudzionetse wekha kwa wansemble, nupereke nsemble ya pa cikonzedwe cako, monga adalamulira Mose, kukhale umboni kwa iwo. (Luka 5:14)**

### **KODI ACHITE CHANI NGATI SANACHIRITSIDWE:**

Musalore kuti anthu akhumudwe chifukwa sanachiritsidwe. Pewani kupeza chifukwa chomwe chachititsa kuti asachiritsidwe (pokhapokha ngati Mulungu wamvumbulutsa mwapaderadera). Asanayambe kupemphera auzeni popeza sanawone zotsatira ndi maso awo zotsatira izi sizikutanthauza kuti sanachiritsidwe. Machiritso amayambiri ku uzimu. pali machiritso ochedwerapo, monga ngati machiritso akusabereka kwa Abrahamu ndi Sarai, ngakhale kuti Mau anaperekedwa pakalebe.

Komaso nthawi imakhudwidwa. Tamuganizireni munthu wolumala pa chipata chakachisi pa Machitidwe 5. Yesu amkadutsa pachipata chakachisicho nthawi zambiri, koma timauzidwa kuti munthu wolumalayu anakhalapo kwa zaka zambiri. Mmalo mwake anazachiritsidwa ndi Petro ndi Yohane patsogolo (Machitidwe 5:15-16). Panalinso nthawi yoyikika pa nkhani ya Yobu ndi Lazar.

Mwina mukhoza kufuna kuika munthu woti azigwira ntchito yolondola antthu odwala potsatira ndondomeko zotsatirazi:

1. Pitirizanibe kukakamira mupemphero la machiritso: Yesu anaphunzitsa kukakamirabe mupemphero. Iye sanaletse kutero. Itanani akulu ampingo kuti azakupemphereni.
2. Pitirizanibe kumanga chikhulupiriro chanu: Muntha kuchita zimenezi pophunzira “Rhema” Mau a Mulungu amachiritso.
3. Pitirizanibe kumvomereza machimo anu: vomerezani machimo anu tsiku ndi tsiku kuti asawononge nthupi lanu. Khalani ndikuyenda mkumvera kwa Mau a Mulungu.
4. Gwiritsani ntchito mphamvu zanu za uzimu: Okhulupirira onse ali ndi maziko a machiritso ndi mamasuridwe. Yambani kuwagwiritsa ntchito. Izi ndi:
  - Mau a Mulungu.
  - Mwazi wa Yesu.
  - Mau a umboni wanu.

- Ulamuliro womanga kapena kumasula.
  - Pemphero ndi matendo.
  - Zida zakhondo zomwe ziri pa Aefeso 6:10-18.
  - Ulamuliro ndi mphamvu ya Mzimu Woyera.
5. Ngati pali poyenera, sithani kakhaliidwe ka moyo wanu: Chotsani chikhaliidwe chonse chauchimo ndi chosayenera. Machiritso amchitika pamene mukukhala mogwirizana ndi kumvera Mau a Mulungu.
  6. Tsatirani malangizo a M'malemba a moyo ndi kukhala mwathazi.
  7. Khalani pamalo achikhulupiriro: zunguliridwani ndi malo omwe machitachita ake ndi achikhulupiriro pokhala mbali imodzi yamkumano wa okhulupirira.
  8. Ziperekeni nokha kwa nthunthu kwa Mulungu: Chikhulupiriro chathunthu chimatanthauza kuti pakukhala moyo kapena kumfa, matenga kapena moyo wanthazi, madziwa kuti muli mmanja mwa Mulungu. Yohane 10:29; Yobu 13:15; 19:26.
  9. Khalani odekha pakuzuzika: Pamene mukudikira machiritso amphumphu, khalani modekha pakuzuzika kwanu mu njira yakuti ena azakopeka nawo. Mukhoza kuchita choncho pochita izi:
    - Kuyamika: 1 Atesalonika 5:16-18.
    - Kulola Mulungu kuti awonetsere mphamvu Yake mchifoko: 2 Akorinto 12:9-10.
    - Kukhala odekha pamene mukudikirira. Anthu amadikira zotsatira zazoyezedwa zawo mu ofesi ya dotolo. Timadikira kuti makhwala agwire ntchito. Nchifukwa chani sitimadikira pa Mulungu? Onse amane ali odekha amalandira malonjezano: Ahebri 6:12; 12:2; Yakobo 1:2-4; 5:10-11; Masalimo 27:14; 37:34; Yesaya 40:31; Aroma 5:3-5.
    - Zindikirani kuti palibe kuzuzika kopanda cholinga: werengani zomwe Baibulo linalamba za onse omwe anazuzikapo.
  10. Tengani malonjezano a Mulungu: Ngakhale pomwe mukuwona ngati kuti Mulungu wakusiyani, pitirizanibe kukumbutsa malonjezano ndi kupemphera mapemphero awa: Masalimo 5:1-3; 6:2-9; 13:1-6; 22:19; 27:7; 31:21-22; 42:9-11; 54:1-2; 55:1-2; 70:1; 71:9-21; 86:6-7; 94:19; 102:1-7; 2 Akorinto 4:17-18.
  11. Patsani ndipo muzalandira: Baibulo limaphunzitsa ndondomeko yofunikira kwambiri yamuufumu wa Mulungu ndiyakuti timalandira pamene tapereka. Ngati ndinu

okhulupirira, yambani kutumikira mphamvu yamachiritso a Mulungu kwa ena.  
Pamene mukupereka, muzalandira.

## MAYESO OZIYENSA NOKHA

1. Lembani veis yotsogolera.

---

---

---

2. Fotokozani zokozekera zoyamba pa utumiki wamachiritso.

---

---

---

3. Lembani mwachidule ndondomeko zazotumikira machiritso.

---

---

---

4. Fotokozani chisamaliro chowatsatira kwa onse omwe sanachiritsidwe.

---

---

---

5. Fotokozani chisamaliro chowatsatira kwa onse amene sanachiritsidwe,

---

---

---

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli.)

## ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Onani zitsanzo za Yesu kufunsa mafunso kwa odwala asanatumikire machiritso:
  - Marko 5:1-20                      Yesu anafusa munthu wogwidwa ndi ziwanda.
  - Marko 8:22-26                      kufunsidwa kwa munthu wosawona.
  - Marko 9:14-27                      Mafunso okhudzana ndi nyamata wamizimu yoyipa.
  - Marko 10:46-52                      Mafunso okhudzana Batuneyo wakhungu.

2. Nazo mwa chisamaliro chotsatira kwa utumiki wa machiritso:

Siyani mmanja mwa Mulungu zotsatira. Musamadere nkhwawa pa zomwe zingachitike ngati zingalephereke. Mungakhale bwajji inu wolemphera pamene amachiza ndi Mulungu? Simatenga matamando chifukwa cha machiritso owoneka amachiritso akumwamba, kodi matero? Nanga nchifukwa chani kuzitenga kukhala wolakwa pamene palibe zotsatira zowoneka?

Pokhapokha ngati Mulungu angawonetsere chifukwa cheni cheni chimene chapangitsa kuti pasakhale zotsatira zowoneka, musiyereni Mulungu mafunso osayakhidwa (Deuteronome 29:29). Musamayesere kupeza zifukwa kapena kuweruza komwe kumachokera munzeru zamunthu wosalungama. Kumbukirani tchimo loyamba la munthu linali lofuna kukhalangati Mulungu pofuna kudziwa zinthu zonse. Mvomerezani kudadwitsa kwa Mulungu kukhala mbali imodzi ya moyo.

Madotolo amagwira ntchito ndizipangizo zapamwamba mmanja mwawo. Nthawi zina wodwala samachira, koma madotolo samaleka kuchita ntchito yawo ngati wodwala wamwalira. Kodi sitingachitenso chimodzimidzi ndi zipangizo zimene Mulungu watipatsa-kupitiriza kuzigwiritsabe ntchito ndi kukula muutumiki wamachiritso posatengera zolephera zina?

Nthawi zonse kumbukirani: Zotsatira zowoneka ndi mason ndi zodzbwitsa, koma zinthu zamuyaya ndi zonse zimene sizimawoneka. Ichi nchifukwa chake Yesu anati kwa ophunzira Ake pamene amkaika chidwi chawo pazotsatira pakulalika kwawo ndi kuchiritsa:

**Koma musakondwera nako kuti mizimu idakugonjerani, koma kondwerani kuti maina anu alembedwa m'Mwamba. (Luka 10:20)**

3. Gwiritsani ntchito ndandanda omwe ungakuthandizeni kuti mutumikire kwa anthu omwe adwalika kwambiri:
  - I. Pali matenda otengera kuimfa: Pa Yohane 11:4 Yesu anati matenda a Lazaro sanali omutengera ku imfa. Izi zikutanthauza kuti pali matenda ena omwe amatengera ku imfa.

II. Pali mitundu iwiri ya imfa yachilengedwe:

- A. Imfa yobwera mwachangu: Imawononga nthupi kuti mzimu ukapululumuke.
- B. Imfa yololezedwa: Chifukwa chazochitika zazochitika za moyo zachilengwe (Ahebri 9:27; Mlaliki 3:2; 2 Mafumu 13:14; Yesaya 38; 2 Mafumu 20)

III. Cholinga chamachiritso sikuthauza kuti sitizafanso:

- A. Ngakhale amene Yesu anawaukitsa kwa akumfa pamapeto Pake anazamwaliranso.
- B. Anthu ena amasungidwa mwa umulungu kuzotsatira za ukalamba monga momwe analiri Mose. Ena amatsata njira ya chilengedwe yaukalamba, monga momwe analiri Yoswa.
- C. Baibulo silinalonjeze kusamwalira padziko pano ngati mbali imodzi yapangano lamachiritso. Musazunguzike pamene Khristu amene wakhulupirira ndikulandira machiritso akumwamba kumatenda kenako mkumwalira. Izi zinachitikanso kwa Elisa, koma zaka zambiri mafupa ake anali ndi mphamvu yodzutsa munthu womwalira. Izi zikutathauza kuti sikuti anamwalira chifukwa chosowa chikhulupiriro!

IV. Pamene mukutumikira kwa munthu wodwalika kwambiri muzifusa nzeru kwa Mulungu: Kodi ino ndi nthawi yoyikika ya munthuyu kuti amwalire?

- A. Ngati Mulungu angavumbulutse kuti ndi nthawi yoyikika, nde athandizeni kuti akozekere monga ngati mmene Yesu anachitira ndi mbava zija pa mtanda.
  - 1. Mukhatsimikizike kuti akumudziwa Yesu monga mpulumutsi wawo.
  - 2. Ngati ali okhulupirira, onetsetsani kuti palibe tchimo limene sanalape.
  - 3. Alimbikitseni kuti aike zochita zawo mmalo mwake.
  - 4. Alimbikitseni kukoza maubale ngati panali mavuto pakati pa iwo ndi anthu ena.
  - 5. Athandizeni kumvetsetsa kut imfa imabwera kwa wina aliyense: kwa okhulupirira, imfa mkati mwa moyo wosatha tinali nawo kale. Tikuyenera tisi the mawonedwe anthu. Sitikuyenera kusaka imfa. Kusowa kunthupi ndekuti mkukhala ndi Ambuye (2 Akorinto 5:8). Imfa ndi mdani, ndipo ndi mdani womaliza yemwe azawonongedwe (1 Akorinto 15:26). Kuukitsidwa kwa Yesu chinali “chipatso choyamba” kuwonetsera imfa yagonjetsedwa koma sinawonongedwe. Ndi khondo ya mdaniyi yomwe imawalanda zida okhulupirira (1 Akorinto 15:55).
  - 6. Athandizeni kumvetsetsa kuti Mulungu ndi wamphamvu zonse. Akhonza kulowerera nthawi ina iliyonse mkuwapangitsa iwo kuti akhale ndi moyo wautali.



7. Akumbutseni iwo kuti imfa ndi machiritso omaliza. Sipamakhalanso ululu uliwonse kapenaso kudwala. Timalowa mkupezeka kwa Mulungu mwamphumphu. Kudwala kuli ngati tchimo. Tinapulumsidwa kuchilango cha tchimo (kudwala) pamene tinalandira Yesu kukhala Mpulumutsi ndi Mchiritisi. Tikhoza kupitirirabe kumasulidwa kumphamvu yake monga ngati okhulupirira, koma mtsogolo pamene tizapite kukhala ndi Ambuye. Mulungu ali ndi njira yotembenuza zinthu zomwe satana anazikonza kuti zikhale zoipa koma Iye amazisitha mkukhala zabwino. Imfa chinali chilango cha tchimo, koma chifukwa cha imfa Yesu inabweretsa moyo. Ichi nchifukwa chake imfa inamezedwa nchigonjetso. Mu imfa, Mulungu amabweretsa machiritso amuyaya.
  8. Aike chidwi chawo pa moyo wamuyaya ndi chiukitso. Gwiritsani malemba otsatirawa: Yohane 11:5-6; Yobu 19:25-27; Aroma 8:10-11, 17-18, 22-23; 10:11; 1 Akorinto 15:42-44, 54-58; 2 Akorinto 4:16-18; 5:1; 1 Atesalonika 4:13-18.
- B. Ngati simunalandire Rhemah mau a Mulungu ngati iyi iridi nthawi yake yoyikika ya imfa.
1. Pitirizani kupempherera machiritso molingana ndi chifuniro cha Mulungu. Izi sizifuna njira zanthu, koma kumulola Mulungu kuti achite malingana ndi chifuniro Chake, kuti kaya awatenga iwo kapena azawaukitsa. Mkofunikaso kupemphera mu Uzimu, popeza Mzimu Woyera amadziwa chifuniro cha Mulungu ndipo azapemphembedzera moyenerera (Aroma 8:26).
  2. Alimbikitseni odwala kuti azipereke okha kuthuthu pokhulupirira Mulungu, kaya pokhala ndi moyo kapena pakumwalira. Yohane 10:29; Yobu 13:15.

## CHAPUTALA 19

### “PAMENE MUKUMUKA, KAMASULENI”

ZOLINGA:

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba Vesi yotsogolera wosawonera.
- Kuwonetsera magulu atatu aziwanda amene amachitira chiwembu nthupi, moyo, ndi mzimu wa munthu.
- Kufotokoza kufunika kwa mzimu wozindikira mizimu pothana ndi mphamvu yaziwanda.
- Kufotokoza tanthauzo logwidwa ndi ziwanda.
- Kuwonetsera machitidwe a munthu yemwe wagwidwa ndi ziwanda.
- Kufotokoza tanthauzo lakugwidwa ndi ziwanda.
- Kuwonetsera machitachita a munthu yemwe wagwidwa ndi ziwanda.
- Kulemba mwachidule utumiki wa Yesu pokhudzana ndi mphamvu ya ziwanda.
- Kugwiritsa ntchito ndondomeko za mmalemba pogonjetsa mphamvu ya ziwanda.

**VESI YOTSOGOLERA:**

**Za Yesu wa ku Nazarete, kuti Mulungu anamdzoza iye ndi Mzimu Woyera ndi mphamvu; amene anapitapita nacita zabwino, naciritsa onse osautsidwa ndi mdierekezi, pakuti Mulungu anali pamodzi ndi iye. (Macitidwe 10:38)**

### MAU WOYAMBA

Kwanthawi yayitali ntchito ya ziwanda yakhala ikutsutsidwa ndi anthu ambiri kukhala machitachita achikhalibe achikunja. Sizinatengwe kukhala mvuto lomwe limalowa miyoyo, makomo, makachisi, ndi maiko. Koma anthu ngati inu omwe akuzuzidwa, kuvutitsidwa, ingakhaleenso kulowedwa ndi mphamvu yakumidima yomwe imadziwika kuti ziwanda. Yesu anatomikira kwa onse amene anakhudzidwa andi mphamvu ya ziwanda (Machitidwe 10:38) ndipo analamula omutsatira Ake kukachita chimodzi modzi pamene amkafalitsa Uthenga Wabwino wa Ufumu (Mateyu 10:1).

Chaputala chino chikuwonetsera ndondomeko zakutumikira kwa onse omwe akhudziwa ndi mphamvu ya ziwanda. Kuti akalandire Uthenga Wabwino akapolo amenewa koyambirira akuyenera kumasulidwa kumsingazo. (Sukulu ya Harvest Internation iri ndi phunziro lotchedwa “Ndondomeko za Uzimu: *Buku la nkondo ya Uzimu*: lomwe limapereka ndondomeko wa machitachita a satana ndi mphamvu ya ziwanda. Ngati simukudziwa za nkondo ya uzimu, mukuyenera kupeza buku limenero musanayambe utumiki wamamasuridwe.

**YESU NDI ZIWANDA**

Kuphunzitsa ndi utumiki wa Yesu unawonetsera kuti mizimu yaziwanda ndi mphamvu yazoipa zeni zeni. Zomwe Yesu anaphunzitsa zokhudzana ndi ziwanda ndi momwe anathanirana nazo zimapereka uthenga wamachitachita a satana.

Yesu anamvomereza kuti satana ndi olamulira wa ziwanda. Anaphunzitsa zowona zake za mphamvu ya ziwanda. Iye anati kutulutsa ziwanda ndi chizinfikiro chimodzi chosonyeza kuti Ufumu wa Mulungu wabwera. (Werengani Mateyu 12:22-30, Marko 3:22-27, ndi Luka 11:14-23 pachidule cha zomwe Yesu anaphunzitsa zokhudzana ndi ziwanda.)

Mbali yayikulu ya utumiki wa Yesu unakhudza pothana ndi ziwanda. Ndi chitsanzo cha Yesu ndi ulamuliro wa dzina Lake omwe umapereka maziko a Malemba othanirana ndi mphamvu ya ziwanda. Yesu anatumikira kwa onse omwe anabwera ndi mvuto laziwanda:

**...Mulungu anamdzoza iye ndi Mzimu Woyera ndi mphamvu; amene anapitapita nacita zabwino, naciritsa onse osautsidwa ndi mdierikezi, pakuti Mulungu anali pamodzi ndi iye. (Macitidwe 10:38)**

Pa “zoonjezera kuphunzira” mbali ya phunziro lino muphunzira zolembedwa zapaderadera za m’Baibulo pomwe Yesu anathanirana ndi mphamvu ya ziwanda.

## **MMENE ZIWANDA ZIMAGWIRIRA NTCHITO**

Ziwanda zimagwiritsidwa ntchito ndi satana kutsutsana ndi Mulungu, zolinga Zake ndi anthu Ake. Amamenyaso nkondo ndi anthu osakhulupirira kuti asadziwe choonadi cha Uthenga Wabwino. Ziwanda zimatenga ulamuliro wadera lina (maulamuliro) monga ngati kalonga waku Pereza yemwe anatchulidwa mu Daniel 10:12-13. Ziwanda zimagwiranso ntchito kupyolera mpakukhala ngati anthu, mwa amuna ndi akazi, pokakwaniritsa zolinga za satana pa dziko.

Kutsutsana ndi chifuniro cha Mulungu nde cholinga chachikulu chasatana. Mau oti “satana” matanthauza kuti “mdani.” Satana ndi mdani woyamba wa Mulungu (Yobu 1:6; Mateyu 13:39). Munthu ndi mdani wake wachiwiri (Zakariya 3:1; 1 Petro 5:8).

Ziwanda ziri ndi mawonekedwe osiyanasiyana. Chiwanda china chinazifotokoza chokha mu 1 Mafumu 22:23 monga ngati mzimu wabodza. Mzimu wosamva ndi wosayakhula unatchulidwa mu Marko 9:25. Ziwanda zamawonekedwew osiyanasiyana zimagwira ntchito ngati mizimu yobweretsa zowawa, mizimu yopangitsa chigololo, ndi mizimu yonyasa. Satana amazigwiritsa ntchito polimbana ndi munthu kunthupi, moyo ndi mzimu.

## **MIZIMU YA ZIFOOKO:**

Iyi ndi mizimu imene imazuza matupi a anthu okhulupirira ngakhalenso osakhulupirira. Werengani Luka 13:10-17. Mzimayi ameneyu anazuzidwa ndi mzimu wa zofoka. Anapezeka pa tsiku la sabata ndi Yesu anamuitan iye kuti “mwana wamkazi wa Abrahamu.” Mfundo zonsezi zikuwonetsa kuti iye anali wotsatira Mulungu, koma nthupi lake linazuzidwa ndi satana kwa zaka zisanu ndi zitatu. (Zitsanao zina za mphamvu ya ziwanda yomwe imazuza nthupi onani Mateyu 12:22; 17:15-18; Machiritso 10:38; 2 Akorinto 12:7.)

## **MIZIMU YOKOPA PONYENGERERA:**

Mizimu imeneyi imazuza mzimu wa munthu, kumukopa iye kuti akhulupirire chiphunzitso chonama, kuti akalandire chilango chosatha kumapeto kwake. Ndimizimu yaziphunzitso chonyenga, Akhristu onama ndi aphunzitsi onyenga:

**Koma Mzimu anena monenetsa, kuti m' masiku otsiriza ena adzataya cikhulupiriro, ndi kusamala mizimu yosoceretsa ndi maphunziro a ziwanda. (1 Timoteo 4:1)**

**Pakuti ali mizimu ya ziwanda zakucita zizindikilo; zimene zituruka kumka kwa mafumu a dziko lonse, kuwasonkhanitsira ku nkondo ya tsiku lalikuru la Mulungu, Wamphamvuyonse. (Cibvumbulutso 16:14)**

**Ndiye amene kudza kwace kuli monga mwa macitidwe a Satana, mu mphamvu yonse, ndi zizindikilo ndi zozizwa zonama.**

**Ndi m' cinyengo conse ca cosalungama kwa iwo akuonongeka, popeza cikondi ca coonadi sanacisandira, kuti akapulumsidwe iwo. (2 Atesalonika 2:9-10)**

Mizimu yokopa mkuphatikizapo mzimu wa zamaula omwe unatchulidwa pa Machitidwe:

**Ndipo panali, pamene tinalinkunka kukapemphera, anakomana ndi ife namwali wina amene anali ndi mzimu wambwebwe, amene anapindulira ambuye ace zambiri pakubwebweta pace. (Macitidwe 16:16)**

Mizimu yamaulayi kapena “mizimu yachizolowezi” imagwira ntchito mwa amaula, amfiti, ndi owombeza ndi anyanga. Kupyolera munjira yosakhala yammalemba mizimu yam aula imatha kunena zakutsogolo kapena kuzindikira nzeru zomwe zimadziwika mwachilengedwe. Machenjezo okhudzana ndi mizimu yachizolowezi aperekedwa pa Levitiko 19:31; 20:6; Deutoronome 5:9; 18:10; Levitiko 20:7; ndi 1 Samueli 28:3.

Mizimu yonyengerera imatha kuwona chikumbumtima, kukopa, kunyengerera, kuika chidwi, kusangalatsa, kumutsa mudyo, kukopa, ndi kunyenga. Mizimu yonyengerera ndi yachangu pochititsa “kuika kwa uzimu mmalo akuluakulu.” Nthawi zonse imakhalapo ndipo imagwira ntchito zipembedzo zokana Yesu ndi paliponse pamene chiphunzitso chonyenga chikuchitika. Kumbukirani kuti satana amafuana kulambiridwa ndipo akhoza kutenga kulikonse komwe angawapeze. Mizimu yokoka imanyengerera amuna ndi akazi kuti azilambira mafano ngakhalesnso satana amene.

### **MIZIMU YONYANSA:**

Mphamvu yaziwandayi imazuza moyo wa munthu. Imakhudzidwa ndi makhalidwe achigololo, maganizo onyasa, kusaupeza mtima ndi machitachita ena ausatana omwe amagwiritsidwa ntchito kumanga amuna ndi akazi. Pamene satana akumulamulira munthu ndi mizimu yonyasa, amagwirisa ntchito mmakomo, makachisi, ndi padziko lonse popeza malo onsewa makhala anthu. Umu ndi mmene satana amagwirira ntchito madela osiyanasiyana. Zitsanzo za mizimu yonyasa onani Mateyu 10:1; 12:43; ndi Mark 1:23-26.

### **KUPONDEREZA, KULALAMULILIDWA, KULOWEDWA**

Mizimu yoyipa imatha kumapondereza anthu. Kupondereza kumatanthauza kuti kukakhali pansu, kulimbana, kapena kukutsekera kunja. Kupondereza kumeneku kumatsatana ndi mizimu yoyipa mu njira zambiri. Imabweretsa kukhumudwa, imapanga nyengo zonyasa, ndipo imapereka malingaliro oipa monga maganizo ofuna kuzipha, chigololo, kusakhulupirira, matha, ndi zina zambiri. Ziwanda zimalenga machitachita awusatana.

**Za Yesu wa ku Nazarete, kuti Mulungu anamdzoza iye ndi Mzimu Woyera ndi mphamvu; amene anapitapita nacita zabwino, naciritsa onse osautsidwa ndi mdierekezi, pakuti Mulungu anali pamodzi ndi iye. (Macitidwe 10:38)**

Ziwanda zimatha kulowaso anthu. Kulowedwa ndi ziwanda ndi nyengo imene chiwanda ndi nyengo imene mizimu yoyipa (ziwanda) zimalowa ndi kumakhal mu nthupi la munthu ndipo zimatenga ulamuliro wamunthuyo kwanthuthu konse. Anthu ena amakonda kugwiritsa ntchito mau akuti “kulumulidwa ndi ziwanda” osati kugwidwa ndi ziwanda, koma mosataterenga dzina lomwe likugwiritsidwa ntchito, munthu wolowedwa ndi ziwanda ndi yemwe amakhala nyumba yokhalamo ziwanda. “Kulowedwa” sizikutanthauza kuti munthu alibe udindo pamachimo ake. Udindo wake ndi umene wachititsa kuti allowedwe ndi ziwanda.

Kulowedwa kukhoza kuchita mochita kufuna. Munthu antha kufuna kulowedwa ndi mphamvu ya mizimu ndicholinga chakuti azitha kuwona zakutsogolo, kutemberera, kuti akhale mfiti, komaso kuti akhale ndi mphamvu zodabwitsa. Kulowedwa kukhozaso kuchitika mosafuna. Munthu oti sanafune kuti allowedwe, koma kupyolera mmalingaliro awuchimo, machitidwe, kapena kuyanjana ndi anthu aziwanda kukhoza kumpangitsa munthu kuti allowedwe ndi ziwanda.

Mphamvu ya ziwanda imagwira ntchito mwamakolo ndipo machimo amakolo atha kukhudza m'bado winawo (Onani Eksodo 20:5; 34:7; ndi Deutoronome 5:9). Izi zikukamba za kulowedwa ndi ziwanda kapena kuponderezedwa kwa ana monga momwe zinalmbedwera pa Marko 7:24-30 ndi 9:17-21.

### **KODI ZIWANDA ZIMAKHUDZANSO OKHULUPIRIRA?**

Okhulupirira weniweni sangalowedwe ndi ziwanda chifukwa Mzimu Woyera sungakhale mu kachisi chimodzi ndi mzimu woyipa.

**Kapena simudziwa kuti thupi lanu liri kacisi wa Mzimu Woyera, amene ali mwa inu, amene muli naye kwa Mulungu?**

**Ndipo simukhala a inu nokha. Pakuti munagulidwa ndi mtengo wace wapatali; cifukwa cace lemekezani Mulungu m'thupi lanu. (1 Akorinto 6:19-20)**

Pamene uli wakwa Mulungu ndipo wadzadzidwa ndi Mzimu Woyera, sungakhalenso wasanatana mkudzadzidwaso ndi mizimu yake pa nthawi imodzi. Mzimu Woyera sangakhale pamalo amodzi mkachisi imodzi ndi satana.

Koma izi sizikutanthauza kuti okhulupirira sangakhudzidwe ndi mphamvu ya ziwanda. Ndi mphamvu yomweyi imene timakhala tikulimbana nayo. Satana amagwiritsa ntchito mphamvu ya ziwanda pochitira ziwembu okhulupirira kuchokera kuja popyolera

kuwapondereza, zizindikiro za zimenezi zinakambidwa kale pambuyo. Koma sizingalowe mwa okhulupirira weni weni. “Kulowedwa” kumawonetsa kukhazikika mkati. “Kupondereza” kumasonyeza zochochela kunjira. Machitachita a okhulupirira akhoza kukhala ausatana ngati angalole kuti mphamvu ya ziwanda iwapondereze. Kuponderezedwa kotereku ndi mphamvu yoyipa kumampatsa mpata satana kuti awagwiritse ntchito pa zolinga zoyipa.

Izi ndi zomwe zinachitika pamene Petro, ophunzira wa Yesu, anagwiritsidwa ntchito ndi satana pofuna kumuletsa Yesu kukamva zowawa chifukwa cha machimo a anthu onse. Pamene Yesu ananena za mazunzo amene azakumane nawo, Petro anati:

**...Dzicitireni cifundo, Ambuye; sicidzatero kwa Inu ai. (Mateyu 16:22)**

Yesu anati kwa Peturo

**...Pita kumbuyo kwanga, Satana iwe; ndiwe condikhumudwitsa Ine; cifukwa sumasamalira za Mulungu, koma za anthu. (Mateyu 16:23)**

Sikuti Yesu amkatanthauza kuti Petro ndi satana. Anazindikira kuti pa nthawi imeneyo Petro anamulola satana kuti agwire ntchito kupyolera mwa iye. Sikuti analowedwa ndi ziwanda, koma analola kuti mizimu ya satana kuti imugwiritse ntchito. Kupyolera mu zochita zawo, okhulupirira “amampatsa mpata” (kupereka mwayi) kwa satana kuti awagwiritse ntchito (Aefeso 4:27)

Pamene munthu wabadwanso mwatsopano, dzina lake limalembedwa mu buku lapaderadera ku Mwamba lomwe limatchulidwa kuti buku la moyo. Okhawa amene maina awo ali m’buku limeneri ndamene adzakakhale Kwamwamba kwa muyaya:

**Ndipo ngati munthu sanapezedwa wolembedwa m’buku la moyo, anaponyedwa m’nyanja yamoto. (Cibvumbulutso 20:15)**

Zoteka dzina lanu kulembedwa m’buku lamoyo, koma keneko mkufufutidwamo chifukwa chobwerera ku moyo wauchimo:

**koma 4 ndipumpuatha thupi langa, ndipo ndiliyesa capolo; kuti, kapena ngakhale ndalalikira kwa ena, ndingakhale votayika ndekha. (1 Akorinto 9:27)**

Paulo anazindikira kuti tchimo. makamaka machimo osalapa akuthupi, kukhoza kuchititsa kuluza moyo wake womwe ngakhale analalikira kwa ena.

Popitiriza kukhalabe mu uchimo kumachititsa kumapangitsa kubwerera mbuyo. Izi zikutanthauza kuti simakhalanso okhulupirira Yesu Khristu weni weni. Ngati mupitirizabe kumachimwacew mwadala ndi kusamalapa, palibe amene azakuzuni kuti malekera pati kukhala otsatira wa Yesu ndipo makhalano mbali imodzi ya ufumu wa satana. Ndi Mulungu yekha amene angadziwe malire anu. Koma zimenezi zikachitika, makhala kuti mwatsegula nokha nkhomo kwa mdaniyo, kuphatikizapo kupereka mwayi oti ziwanda zikuloweni. Ndi chifukwa chake kuli kofunika kwambiri kuti mukachimwa muzilapa mkubwereranso kunjira yachiyero:

**Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutasambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse. Tikanena kutasitidacimwa, timuyesa iye wonama, ndipo mau ace sakhala mwa ife. (1 Yohane 1:9-10)**

Yesu amatchulidwa kuti Mau a Mulungu mmalo ambiri m'malemba. Ngati Mau a Mulungu sakhala mwa inu, ndekutiso Yesu sakhala mwainu.

## **MMENE ZIWANDA ZIMATENGERA ULAMULIRO**

Ziwanda zimatenga ulamuliro munjira zambiri:

- 1. Kupyolera kumibado:** Ziwanda zikhoza kupondereza kapena kumulowa munthu chifukwa cha chakulowedwa ndi kuponderedwa kwa makolo kalelo. Izi zimapangitsa kuti ziwanda zizigwiranso ntchito mwa ana (Eksodo 20:5; 34:7; Deutoronome 5:9).
- 2. Kupyolera malingaliro:** Mmalingaliro ndi malo amodzi akulu amene asatana amakondamo kumenenya nkhondo. Ngati satana angalamulire maganizo anu, mapeto ake azatenganso ulamuliro wazochita zanu. Kusowa koteteza malingaliro anu kuzapangitsa kuti muzilephera kukganiza bwino komwe kumapangitsa kuti muzingochita uchimo. Kupitiriza kumangochimwa mmaganizo ndi muzochita kukhoza kupangitsa kuti muponderezedwe komaso mulowedwe ndipo pamapeto pake muzakhala ndi maganizo ozunguzika monga mowe amanenera pa Aroma 1. Awa ndi maganizo amene akugwiritsidwa ntchito ndi satana. ziwanda zimapezaso danga kupyolera mmalingaliro kupyolera kuika makhwala ozunguza bongo amene amachepetsa kaganizidwe kokaniza ziwanda ndipo zimakhala ndi mwayi wolowa kwambiri.
- 3. Kupyolera machitachita auchimo:** Maganizo auchimo posakhalitsa amadzadzidwa ndi machitachita auchimo. Mwachitsanzo, maganizo achigololo amakwaniritsidwa pokachitadi chigololocho. Tchimo ndikuwukira, ndipo ndimaganizo owukira ndipo machitamachita ake amaperaka mwayi oti machitachita aziwanda alowere.

Osakhulupirira amene akukhala mu uchimo amatsegula khomo osati kwa kupondereza kokha kwa mphamvu ya ziwanda, komaso kulowedwa. Pakhondo ya uzimu palibe yemwe amangokhala osatenga nawo mbali. Makhala kuti muli kumbali yabwino kapoena yoyipa. Makhala wakwa Mulungu kapena kwa satana. Ngati muli wa satana ndipo simunabadweso mwatsopano mwa Yesu Khristu, ndekuti ndinu wake kuti akugwiritseni ntchito, kuponderezedwa, kapena kulowedwa monga momwe afunira.

- 4. Kupyolera kufuna:** Anthu ena amachita kufuna kukhala pansu pa ulamuliro wa mphamvu ya ziwanda. Amachita izi ndi zolinga zokhala ndi ndimphamvu zoopsyasochitira zinthu zoopsyaso.
- 5. Kupyolera mu nyumba yopanda anthu:** Ziwanda zimayensa nthupi la munthu mokhalamo mwawo (Mateyu 12:44). Pamene amunthu wamasulidwa ku mphamvu ya

ziwanda ndipo sanadzadze nyumba yake ya uzimu pokhala wobadwaso mwatsopano ndi kulandiranso Mzimu Woyera, kulowedwa kukhoza kuchitikaso.

- 6. Kupyolera kupatsidwa chilolezo:** Nthawi zina Mulungu amapereka chilolezo ku mphamvu ya ziwanda kuti akakwaniritse zolinga zake zapaderadera. Izi zikhoza kuloledwa kuti kukhala ngati mayesero kwa okhulupirira monga mmene zinaliri ndi Yobu. Zikhozasa kukha; la chiweruzo cha tchimo monga mmene zinaliri ndi mfumu Sauli.

### **NDINDANI AMENE ANGATHANE NDI MPHAMVU YA ZIWANDA?**

Kuthana ndi mphamvu ya ziwanda sintchito yowasiyira atumiki otchuka. Yesu anati okhulupirira onse alimkuthekera kugonjetsa mphamvu ya ziwanda:

**Ndipo zizindikilo izi zidzawatsata iwo akukhulupirira; m'dzina langa adzaturutsa ziwanda... (Marko 16:17)**

Yesu anawapatsa omutsatira Ake kuthekera kothana ndi mphamvu ya ziwanda. Koyambirira anapereka mphamvu imeneyi kwa ophunzira Ake:

**Ndipo pamene Iye anadziitanira ophunzira ace khumi ndi awiri, anapatsa iwo mphamvu pa mizimu yoipa, yakuiturutsa, ndi yakuciza nthenda iri yonse ndi zofoka zonse. (Mateyu 10:1)**

**Koma andilambira Ine kwacabe, Ndi kuphunzitsa maphunzitsa, malangizo a anthu. (Buku Lopatulika 1992)**

Anaperekaso mphamvu yomweyo kwa okhulupirira onse:

**Ndipo zizindikilo izi zidzawatsata iwo akukhulupirira; m'dzina langa adzaturutsa ziwanda... (Marko 16:17)**

**Ciritsani akudwala, ukitsani akufa, konzani akhate, turutsani ziwanda: munalandira kwaulere, patsani kwaulere. (Mateyu 10:8)**

Palibe maziko a m'Baibulo oti mkukhulupirira kuti Mulungu amafuna kuti utumiki ofunikawu ungokhala kwa gulu lina la anthu. Munthu wamba wotchulidwa kuti Filipo anagwiritsidwa ntchito ndi Mulungu kutulutsa mizimu yoipa ku Samariya (Machitidwe 8). Komai izi sizikutanthauza kuti okhulupirira akuyenera kuthamanga polimbana ndi mphamvu ya ziwanda popanda kukozeke koyenera, monga momwe ana a Skeva anaziwonera (Machitidwe 19).

Mkufunika kwambiri kuti okhulupirira kuti asamatengeke ndiziwanda. Sitinaitanidwekuti tikazame pa ziwanda. Palibe mpatso ya uzimu yo "tulutsira ziwanda." Koma simukuyera kuwopa mphamvu ya ziwanda. Pamene mwakumana ndi onse amene agwidwa ndi ziwanda, muli ndi mphamvu yobweretsa mamasuridwe ochokera kwa Mulungu.



## KUZINDIKIRA KUPEZEKA KWA ZIWANDA.

Pofuna kugonjetsa mphamvu ya ziwanda, mkoyenera kuzindikira kaye kupezeke kwawo ndi ndale zomwe zimagwiritsa ntchito. Mzimu Woyera wapereka mphamvu ya uzimu yapaderadera yotchedwa “kuzindikira mizimu” (1 Akorinto 12:10).

Kuzindikira kumatanthauza kuti “kubvumbulutsa, kusathula, ndi kusiyanitsa. Mphatso yozindikira mizimu imamphangitsa okhulupirira kukazindikira mizimu imene ikugwira ntchito mwa anthu. Imamulola iye kukazindikira, kusathula, ndi kuloza mizimu yoyipa.

Mphatso yozindikira mizimu ndiyofunika kwambiri polimbana ndi mphamvu ya ziwanda. Imakupangitsani kuti mukazindikire mwachangu ngati munthu ali ndi mizimu yoyipa kapene ayi. Imaletsa kunyengedwa pokopedwa kapena kumizimu yonama. Munthu yemwe ali ndi mphatso imeneyi antha kuzindikira machitachita oipa ndi malingalilo a mohamvu ya ziwanda.

Mwachitsanzo, kusayakhula ndi kusamva kwina (malingana ndizolemba za Baibulo) kumachita ndi mizimu. Kuyakhula ndi kusamva kwina kumakhala zotsatira za ngozi kapene akudwalika. Kuzindikira kumapangitsa kuti mukazindikire choyambitsa chabvutolo komwe kumapereka utumiki wapadera dera.

Sikuti okhulupirira onse ali ndi mphamvu imeneyi yakuzindikira mizimuyi. Ngati okhulupirira alibe mphatso imeneyi pali zizindikiro zakupezeke kwa ziwanda zomwe zingaoneke. Pamene mkazi waku Sumuliko anabwera kwa Yesu mkumpempha Iye kuti amutulutse mwana wake mzimu wonyasa, anati “Mwana wanga wamkazi akuzuzidwa ndi chiwanda” (Mateyu 15:22). Nde anadziwa bwanji izi? Anadziwa izi chifukwa chazizindikiro.

Izi ndi zina mwa zizindikiro zamachitachita a ziwanda:

**Kuloweda ndiziwanda** kumazindikiridwa chifukwa chakusakhazizika ndi zachilendo za ziwanda, satana, kapena zanyanga. Munthu otereyo amatha kuzama mumachitachita azamatsenga ndipo nthawi zonse amapereka ulemu kwa satana kapena ziwanda, kapena amakonda nthawi yake yambiri amakonda kuphunzira mau a satana.

**Kuponderezedwa ndi ziwanda:** Kukhoza kuzindikirika ndizizindikiro zotsatirazi:

1. Kumangidwa kwa kunthupi: “Mwana wa mkazi wa Abrahamu” amene Yesu abvumbulutsa mzimu wozuzidwa anamangidwa kunthupi. Onani Luka 13:10-17. Matenda okhalitsa akhoza kukhala kuponderezedwa ndi ziwanda. Matenda onse sikuti amabwera chifukwa cha mphamvu ya ziwanda. Matenda ena amayamba chifukwa chophwanya malamulo achilengedwe, monga ngati kusadya kosayenera kapena kumwa madzi kolakwika. Matenda ena chimakhala kuti ndi chikwapu. Mfumu ina m’Bainulo imene sinapereke ulemu kwa Mulungu inakathidwa ndi matenda anjoka za mmimba ndipo mapeto ake inamwalira.
2. **Kuponderezedwa kwa ubongo:** Kusokenekera mmaganizo kapena moyo monga ngati kuzuzidwa kwa maganizo, kuzunguzika, kukaika, kudwala matenda oyiwayiwa ndi ena

otero. Kusowa mtendere, kusakwanitsa kuganiza bwino kapena kumvetsera kwa ena, kuyakhula zopanda pake. Mavuto onse amubongo sikuti amayambitsidwa ndi satana. Kufooketsedwa, kuponderezedwa, kusokonekera zikhoza kuyamba chifukwa chodana ndi chakudya china kapena kusakaniza kwa makhwala kolakwika mu ubongo. Mulungu ndiothekera kuchiza mavuto amubongo ndi matenda amene samabwera chifukwa cha mphamvu ya ziwanda komaso ngakhale kubweretsa mamasulidwe pamene ngati abwera ndi ziwanda. Koma tikuyenera kukhala osamalitsa osati kupereka matenda onse kapena mavuto aubongo kuti amayambitsidwa ndi mizimu ya ziwanda. Nthawi zina kusitha kophweka pachakudya ndi machitidwe a moyo kukhoza kuchotsa mvuto ngati layamba chifukwa chakusokonekera kwa nthupi.

3. Mamvuto amaimvaimva: Kusokonekera maimvaimva komwe kumakhalitsa kapena kumazachitikaso, kuphatikizapo kukhumudwa, udani, mkwiyo, matha, kuzivera chisoni, nsanje, kudera khawa, kumva kuti suli otetezeka, kukanidwa ndizita zotero.
4. Mavuto auzimu: Kukhala kuvuta kwambiri kufuna kugonjetsa tchimo, monga ngati chikhaliidwe chauchimo. Kukanizidwa kwa yankho la uzimu kumavuto. Mtundu wina uliwonse wa chiphunzitso chonyenga kapena kunyengedwa, kuphatikizapo kumangidwa ku nsinga waziphunzitso za satana.
5. Zochitika: ziwanda zitha kulenga nyengo yovuta yomwe ndi yopondereza. Nyengo imeneyo kawirikawiri imakhudzana ndi chisokonezo ndipo imatha kuzindikiridwa kuti ndi yaziwanda chifukwa Mulungu siamene amayambitsa chisokonezo (1 Akorinto 14:33; Yakobo 3:16).

**Kugwidwa ndi ziwanda** kukhoza kuzindikirika ndi zizindikiro zotsatirazi:

1. Kudzadzidwa ndi mizimu yonyasa: Izi zimawonetseredwa pochita makhalidwe onyasa. Zikhoza kuphatikizapo kufuna kuyenda opanda zovala. Mwachitsanzo onani Marko 5:2 ndi Luka 8:27.
2. Kukhala ndi mphamvu zodabwitsa: Munthu amawonetsa mphamvu zopitirira muyeso. Mwachitsanzo onani Marko 5:3 ndi Luka 8:29.
3. Kumangozichekacheka: Kuzicheka kumeneku kumatha kutsaganaso ndikutuluka thovu mkamwa. Onani Marko 9:14-29 ndi Luka 8:26-39.
4. Kutsutsa ku zinthu za uzimu: Munkhani ya Pa Marko 6:7 ndi 1:21-28, ziwanda zinamudziwa Yesu ndi masangasanga zinamuza Yesu kuti ziwachokere. Kuopedwa kwa dzina la Yesu, pemphero ndi Mau ndi kunyoza ndizina zonse zomwe ziri za uzimu ndi chizindikiro chakuti munthuyu ali ndi ziwanda. Kunyoza kopitiriza muyezo kukhoza kuzindikirika ndipo kumalamuliridwa ndi zochitika zakunthupi ndi makhalidwe achirendo amasitha pamene zinthu za uzimu zatchulidwa.

5. Kusitha mu chikhalidwe ndi mayakhulidwe: Munthu yemwe amachita manyazi akhoza kusanduka kukhala wachiwawa. Zochitika komaso mawonekedwe amatha kukhuzidwaso. Makhalidwe abwino ndi nzeru zithaso kusitha. Mau amathaso kusitha. Onani Marko 5:9.
6. Kumatsana ndikuzuzika kwakuknthupi: Mukhani yolowedwa ndi ziwanda, izi zimawonekera kwambiri pakuzungizika bongo. (Onani Mateyu 9:33; 12:22; Marko 5:4-5). Zikhozaso kuphatikizapo “kuzichekacheka” kapena kuwonongeka kwa nthupi. (Onani Marko 9:14-29).
7. Kuzivulaza wekha kuthupi: pa Mateyu 17:14 pqli nkhani ya mwana wamamuna wa munthu wina amene amkaziponya yekha pamoto. Pa Luka 8:26-39 munthu ameneyu ogwidwa ndiziwandayu amkazicheka yekha ndi miyala kuzipweteka nthupi lake.
8. Kuzuzika kwakukulu: Luka 8:28 imakamba kuti munthu ameneyu amkayenda mkumalira chifukwa chakuzuzika komwe kumkanchitikira mkati kobwera chifukwa chakugwidwa ndi ziwanda.
9. Kukanika kukhala bwino bwino: Munthu aneneyu amkalephera kukhala bwino bwino muzinda koma amkakhala kumanda. Onani Luka 8:27.
10. Kupyolera kunjira zoti siziri mmalemba: Kuthekera kolosera zakutsogolo kapena kuzindikira zomwe zirisosadziwika. Mkazi wapa Machitidwe 16:16 anali atalowedwa ndi mzimu wonenerera,

Zotsatirazi zikhoza kuwonetsaso kuponderezedwa, kugwidwa ndi kulamulirirdwa ndi ziwanda:

1. Kukhazikika muzonyasa monga ngati kutengpo mbali pakuchita makanema olaula, chigololo, dama, mathanyula, ndi machimo ena achiwerewere. Chilakolako champhamvu pakudya kosayenera, kuzimpha, kuzicheka ndi kupha ena.
2. Kukhala kapolo wa makhwala ozunguza bongo ndi mowa.
3. Masopenya ndi kulingalira komwe sikuchokera kwa Mulungu wowona.
4. Kumangidwa ndi nsinga monga ngati matha, nsanje, udani, miseche, kunyada ndizina zotero.

### **KUTUMIKIRA MAMASULIDWE**

Nazo zina mwandondomeko potumikira mamasuridwe kwa anthu omwe akhudzidwa ndi mphamvu ya ziwanda.

## **KUZIKOZEKERETSA INU MWINI:**

Chikhulupiriro chimadza pakumva Mawu a Mulungu, makamaka “Rhema” (Mawu oyankhulidwa ndi Mulungu). Yambani kumanga chikhulupiriro pamtima panu powerenga Chipangano Chatsopano pokhala ndi malingalironso atsopano:

- Chilichonse chimene Yesu anawauza omutsatira Ake kuti achite, mukuyenera kuyamba kuchita.
- Chilichonse chimene anati Achita, dikirani kuti Azazicitadi.
- Ngati anati mukhoza kumasula onse amene akuzuzidwa ndi satna, nde yembekezani kuwona iwo akumasulidwa.
- Ngati anati kutulutsa ziwanda, nde chitani choncho mu dzina Lake ndipo yembekezani kuti iwo akumverani.

Kanani ziphunzitsa zonse za munthu ndi kusindikira kwanu komwe mulinako. Vomerani kuti Chipangano Chatsopano chimatanthauza zeni zeni zomwe chimanena. Zindikirani kuti ndi chowonadi ndipo chitani moyenera. Ndinu kazembe wa Khristu (2 Akorinto 5:20) kazembe samakayika kuti dziko lomwe lamtumiza kuti akaliyimirire likhala kumbuyo kwa mau ake.

Salani kudy a ndi kupemphera musanayambe kutumikira mamasulidwe. Popeza mphamvu ndi ulamuliro zakumasula zimachokera kwa Mulungu, nde mkoyenera kuti pakhale kulumikizana! Ziwanda zina zimatuluka ndi ndi pemphero ndi kusala kudy a. Yesaya 53 imaphunzitsa kuti Mulungu amalemekeza kusala kudy a komwe kumaika chikwa pazosowa za ena.

## **KUWAKOZEKERETSA ENA:**

Ngati kuli kotheka, gulu la okhulupirira likuyenera kugwiritsidwa ntchito pomanga komaso kutulutsa ziwanda. Yesu anatomiza ophunzira Ake awiriawiri ku utumiki umenewu:

**Ndipo anadziitanira khumi ndi awiriwo, nayamba kuwatumiza Iwo awiri awiri; nawapatsa mphamvu pa mizimu yonyansa. (Marko 6:7)**

Izi sizikutathauza kuti simungatumikire nokha kwa munthu amene wagwidwa ndi ziwanda pamene mwakumkana naye, koma muli mphamvu mugwirizano wa pemphero ndi okhulupirira ena. Popeza mpohamvu zimachokera mugwirizano, nde onse amene akuyanjana nanu mu utumiki wa mamasuridwe akuyenera kukhala okozekera mupemphero ndi kusala kudy a.

Ngati muzakumane ndi munthu amene wagwidwa ndi ziwanda kuti apemphereredwe koma opanda malangizo abwino, ziringati kumukakamiza osakhulupirira kuti amvomere Yesu kuti ndi mpulumutsi wake popanda kuzindikira kuti Iye ndi ndani, zindikirani tchimo ndi kufuna kwawo kwachipulumutso. Pamene mukugawa Uthenga Wabwino wanzeru ofuna kupindula moyo samakakamiza kuti apange chisakho mwachanguchangu. Pali utumiki woyambirira umene ukuyenera kuti uchitiki. Malangizo abwino akuyenera kuperekedwa.

Izinso ziri chimodzimidzi ndi mamasuridwe. Nthawi zina, Mulungu amamasula popanda malangizo oterewa. Koma potumikira mamasuridwe mukuyenera kugwiritsa ntchito njira ina

iriyonse imene inaperekedwa ndi Mau a Mulungu kuti muwone kuti ntchito yagwirika. Chikhulupiriro ndi njira imodzi imene mphamvu ya Mulungu yomasula ndipo imabwera pakumva Mau a Mulungu, nde malangizo ndiofunika kwambiri. Yesu anasakaniza kulalikira ndi kuphunzitsa pamodzi ndi kuchiritsa komaso kumasula ndipo analangiza omutsatira Ake kuti akachitenso chimodzimodzi.

### **MALO OCHITIRAPO UTUMIKI:**

Kutumikira mamasuridwe kwa onse amene akhudzidwa ndi mphamvu ya ziwanda kukhoza kuchitika pa nthawi yomwe mapemphero alimkati mkachisi. Utumiki umenewu sukuyenera kungokhala pamalo obisika basi. Ndi utumiki umene uli wamoyo mu mpingo.

Yesu anatumikira kwa ogwidwa ndi ziwanda monga ngati mbali imodzi ya televizi ya mpingo (Marko 1:21-25). Komabe, sikofunika kuchita kudikira kuti mpingo ukumane kaye kuti munthane ndi mphamvu ya ziwanda. Yesu anabweretsa mamasulidwe paliponse ndi nthawi iriyonse imene wakumana ndi ziwanda.

### **NTHAWI YOTUMIKIRA:**

Pamene mwakonzeka kuti mutumikire machiritso...

#### **1. Yambani kulambira ndi kutamanda:**

Timalowa mukupezeka kwake (pamene pali mamasulidwe ndi machiritso) kupyolera pakulambira ndi kutamanda. Mamasuridwe akhoza kubwera kupyolera pakulambira ndi kutamaba, ngakhale patakhalakuti palibe kutumikira ndi mapemphero chifukwa Mulungu amapezeka mmalambiro a anthu Ake. Pamene tikutamanda, Amapezeka kuti achiritse ndi kumasula.

#### **2. Kukonza malo achikhulupiriro:**

Munayamba kale kuchita izi pamene matumikira Mau a mamasuridwe, koma mukuyenera kutengaso sitepe yowonjezera pokoza malo kukhala achikhulupiriro. Kusakhulupirira kumatchinga ngakhale utimiki wa Yesu ku Nazarete. Nthawi zina Yesu amkathamangitsa osakhulupirira akamatumikira (Marko 5:35-40). Nthawi zina amatha kuwatsogolera anthu kutuluka mmidzi mwawo (munyengo yosakhulupirira) ndicholinga choti awatumikire (Marko 8:23). Mwanengo zina monga momwe Mulungu atatsogolerere, mukuyenera kuwafusa onse omwe akuvutika ndi kusakhulupirira, matha, ndizina zotero... kuti asiye.

#### **3. Yambani ndikupemphera:**

Funsani nzeru ndi chidziwitso musanayambe kutumikira mamasuridwe. Nthawi yamapemphero, Mulungu antha kuwonetsera kwa inu...

- Mau achidziwitso: Mfundo zapaderadera ndi mbiri ya munthu kukhudzana ndi mmene aliri potero ndemuzadziwa kapemphereredwe kake. "Mau a chidziwitso" kukhoza kuphatikizapo kuzindikira mwakuya mu uzimu mwanu, maganizo, mau,

kapena pazويمvaimva. Mau achidziwitso akhoza kubvumbulutsa kuti matendawo ndiotani kapena chifukwa chimene munthuyo ali munyengo imeneyo.

- Vesi yammalemba: Mau a Rhema anyengo imeneyo, munthu kapena gulu.
- Masomphenya: zinthuzi mmaso ammalimgaliro okhudzana ndi yemwe mukumtumikirayo.
- Mau achikhulupiriro: Mau apaderadera achilimbikitso ndi chikhulupiriro chifukwa chamunthuyo.
- Kudzodza kwapaderadera: Kudzadzidwa ndimphamvu mwadzidzi, kumakhala pa mtima, kapena mpamvu zopereka kulimbika mwapaderadera.

#### **4. Funsani mafunso ochepa:**

Izi ndizosafunika. Ndichisakho ndipo zikuyenera kuchitika malingana ndi mmene Mulungu angatsogolere. Mulungu atha kukupatsani mau anzeru mwapaderadera okhudzana ndi nyengo yamunthu ndipo simukuyenera kumufunsaso mafunso.

Koma ngati Mulungu sabvumbulutsa chinachironse kwa inu, musakayike kugwiritsa ntchito njira yofunso mafunso. Yesu anagwiritsa njira zonse yakuthupi ndi yakuuzimu. Pa nthawi zina amkatha kuzindikira nyengo ya anthu ndi Mzimu Woyera. Nthawi zina amkawafunsa mafunso pachomwe akufuna ndi nthawi imene akhalira akuzuzika.

Kufusa mafunso kumakuthandizani kuti mupeze mbiri kuti mukathe kupemphera mwachindunji. Kumakuthandizano kuzindikira ngati munthuyo akufunika malangizo ena musanayambe kupemphera. Yesu amkakonda kuchita zimenezi. Amkawafunsa anthu mafunso okhudzana ndi chikhulupiriro chawo ndipo kenako amathana ndi mphamvu zakusakhulupirira asanawatumikire. Onani zitsanzo zotsatirazi:

- Marko 5:1-20                      Yesu anafusa mafunso munthu waziwanda.
- Marko 8:22-29                    Munthu wosawona anafusidwa mafunso.
- Marko 9:14-27                    Nyamata wamzimu woyipa.
- Marko 10:46-52                    Batumeyo afusidwa mafunso.

Muzimufunsa munthu kuti mvuto ndi chani? Kuyakhula mopempha mwapemphero mkofunika. Yesu anamasula anthu ambiri omwe anadza kwa Iye omwe anamuza zofuna zawo. Kupempha pakokha kulingati kuchita mwachikhulupiriro chomwe chimabweretsa chiyambi chamachiritso (Yakobo 5:14-15). Mukungofuna choonadi chochepa. Simufunika kuti mudziwe mbiri yonse yamoyo yawo.

Mufunsi munthu amene atapemphereredweyo kuti, “Kodi ukukhulupirira kuti Yesu akhoza kukumasula?” Ngati amvomera, nde afunsi kuti,” Mukukhulupirira kuti Yesu antha kuchizi izi pompano?” Ngati yankho lawo ndi “ayi” kumafunso onsewa, pamenepa ndekuti pakufunika malangizo oonjezera ochokera m’Mau a Mulungu.

## 5. Zinfikirani mvuto leni leniro:

Gwiritsani ntchito uthenga omwe mwapeza pa nthawi imene mafunsa mafunso kapena nzeru zimene Mulungu wakupatsani kuti muzindikire ngati mvutolo liri la:

**Lakuuzimu:** Mavuto okhudzana ndi tchimo. Awa amafunika utumiki wa machiritso auzimu (Chipulumutso, kulapa ndi kukhululukidwa kwa machimo).

**Zakunthupi:** Matenda akunthupi amene amayamba ndi kuzuzidwa ndi mizimu yaziwanda.

**Maimvaimva:** Mavuto okhudzana ndi kudera khawa, matha, mkwiyo, kaduka, kukaika, kulephera, nsanje, kuzikonda, kusokonezeka, kukhumudwa, kusakhululuka, zochitika zakale.

Izi zimatchulidwa kuti “machiritso amkati,” koma liwuli lagwiritsidwa ntchito udyo. Sikofunika kubwereranso mbuyo pochita zokozekerra paza mfundo ndi maimvaimva. Sikoyenera kukhala ndi masabata, miyezi, kapena zaka kuti muchiritsidwe kumavuto amenewa. Ngati mungachite zimenezi ndekuti mukuyesera kuchiza munthu wakale mmalo mowathandiza iwe kuti akhale cholengedwa chatsopano mwa Khristu.

Tinayitanidwa kukhala atumiki oyanjanitsa (2 Akorinto 5:18-21). Kuyanjanitsidwa kukuphatikiza kwa Mulungu ndi munthu, ndipo apa mpamene machiritso amkati amabwerera.

Mukuyenera kumuphunzitsa munthu yemwe akufuna kukhululukira. Sikuti ndi:

- Kulungamitsa zolakwa zawina zomwe akuchitirani. (Mwachitsanzo, kunena kuti, ” pochita zimenezi anali atapanikizika.”)
- Sikukana kuti pachiyambi munamvulazidwa.
- Kukana zomwe zinachitidwa kwa inu.
- Kudikira nthawi yochiritsidwa pakumvulazidwa. (Sichoncho).

Kukhululuka kweni kweni kumabwera ndi:

- Kumvomereza kuti zomwe zinachitika kwa inu zinali zolakwika, ndizochita za anthu ochimwa mudziko la uchimo. Sikufunika kubwereraso pambuyo kumakakumbukiranso zomwe zinachitikazo, koma mmalo mwake mukhoza kuthana nazo pozikana. Mvomerezani zomwe zinachitikazi ndi momwe zinakhudzirani.
- Perekani kumvulazidwa kwanu kwa Mulungu ndipo Mumupemphe kuti akuchiritseni kumaimvaimva oipa. Simungaiwaliretu choonadi cheni cheni cha zomwe zinachitika ndi mmene zinakukhudzilani koma chomwe mukufunika ndi machiritso pa zoipa pa zomwe zinakuchitikirani.

- Kumphepha Mulungu kuti akuthandizeni kukhululukira ena omwe anatengapo mbali, nde akhululukireni iwo monga momwe Kristu amakukhululukirani inu. Zindikirani kuti Mulungu akukhululukirani pamene inu mukukhululukiranso ena: “Mutikhululukire ife zolakwa zanthu monga ifenso tikhululukira amangawa anthu.” Munthu akuyeneranso kuzikhululukira yekha (kumva kulakwa pazolakwa zimene wachita) ndipo akuyenera kupempherera machiritso pa maimvaimva ake. Nazo ndondomeko za momwe munthu angazikhululukire yekha:
  - Mvomerezani tchimo lomwe likukupangitsani kulakwa ndi maimvaimva auchimo, mvomerezani kwa Mulungu, ndipo lapani. Mpempheni kuti akukhululukireni machimo anu ndipo achiritse maimvaimva anu.
  - Zindikirani kuti Mulungu akakhululukira, amaiwala (amawaponya kutali machimo anthu monga mmene kuliriri kutalikana kwa kummawa ndi kumadzulo).
  - Nenani 1 Yohane 1:8-9.

**Zamuubongo:** Mavuto ochokera pakuyamba moganiza molakwika, chiwembu cha satana maganizo, kusaganiza bwino. Kumbukirani: chifukwa munthu ndi utatu, nde mavuto ambali imodzi amakhudza munthu yense. Pamene mukutumikira, nthanani ndi munthu yense, osati mbali imodzi yokha. Munthu ndi nthupi, moyo ndi mzimu. Uthuthu ukutanthauza kuti kuthana ndi zonsezi.

#### **6. Zindikirani ngati iri nthawi yoyenera kupemphera:**

Zindikirani ngati iri nthawi yoyenera kapena ayi kupemphera pemphero lamachiritso. Nthawi zina, muzapemphera, koma nthawi zina, musazadabwitsidwe pamene Ambuye azakutsogolereni kuti musapephere kapena muchedwerepo.

Yesu anachedwetsapo machiritso a mwana wa mzimayi waku Sifulina ndi Lazaro. Sanachite ntchito zambiri ku Nazarete chifukwa chakusakhulupirira kwawo. Mulungu atha kukutsogolerani kuti muchedwerepo kufikira atazakupatsaniso malangizo ena, monga ngati akuyenera kuthana kaye ndi mvuto la tchimo, kapena kufuna malangizo ena pamamasulidwe.

#### **7. Pempherani pemphero la mamasulidwe:**

Pempherani pemphero la mamasulidwe lomwe limapita chindunji kumvuto la ziwanda lomwe mwalizindikira. Simukuyenera kumukakamiza Mulungu kuti amasule chifukwa cha pemphero lanu. Monga momwe chipulumutso kuti chilipo kale, zirinso chimodzimidzi ndi mamasulidwe. Monga mmene chiriri chipulumutso kuti chimabwera ndi chikhulupiriro, nde nchimodzimidziso mamasulidwe. Mulungu akufuna kumasula, mangaso mmene amafunira Atapulumsa. Ngakhale kuti mphamvu ya Mulungu nthawi zina imapezeka munjira yapaderadera yomasula (Luka 5:17). Mukhozabe kupitiriza kupemphera popanda kudzodza kwapaderadera kuchita choncho chifukwa Yesu anakulamulani kuti mutero monga mmene Iye anakuzirani kuti mufalitse Uthenga Wabwino.



Gwiritsani ntchito anthu ena kuti akuthandizeni kutumikira ngati muli pa gulu. Pamakhala kuchulukitsa kwa mphamvu ya uzimu pamene anthu ambiri akupemphera pamodzi (Mateyu 18:19).

Yesu ananena kuti koyamba mukuyenera kumanga kaye mdani, kenako nde munthu kumugonjetsa:

**Kapena akhoza bwanji munthu kulowa m'banja la munthu wolimba, ndi kufunkha akatundu ace, ngati iye sayamba kumanga munthu wolimbayo? ndipo pamenepo adzafunkha za m'banja lace. (Mateyu 12:29)**

Ngati mphamvu ya ziwanda yopendereza ndiyochechera kunja, pempherani kuti goli lake liduke ndikutiso kuti mphamvu yawo imangidwe. Mwachitsanzo, Yesu anamasula mzimayi mu Sunagoge ku mzimu wakumva zowawa. Sikuti analowedwa ndi ziwanda, koma anaponderezedwa. Kutulutsa sikunali koyenera.

Ngati nkhani yake iri yolowedwa ndi ziwanda, muli ndi ulamuliro otulutsa ziwanda mudzina la Yesu. Siulamuliro mumphamvu zanu kapena kuthekera kwanu, koma mudzina Lake. Ndikofunika kwambiri kugwiritsa ntchito dzina la Yesu panthawi yakutulusa ziwanda.

Chikhulupiriro, kusala kudya, ndi kupemphera ndizofunika potulutsa ziwanda. (Werengani zomwe zinachitika pa Mateyu 17:4-21). Izi nchifukwa chake kukozechera musanayambe kutumikira mkoyenera. Mau a Mulungu (Aefeso 5:17; Ahebri 4:17); mwazi wa Yesu (Chibvumbulutso 12:11), ndi mphamvu ya Mzimu Woyera (Machitidwe 1:8; 2:38) ndizidaso za mamasulidwe zomwe Mulungu wapereka.

Kuukira kapena kulalatira ziwanda sikofunikira. Ndi udindo wanu mu dzina la Yesu lomwe limachititsa kuti izo zituluke, osati kufula kwa mau anu panthawi ya mapemphero amamasulidwe. Nthawi zonse kanizani kuti ziwanda zikuloweniso. Iri ndi gawo lofunika kwambiri papemphero la mamasulidwe:

**Ndipo pamene Yesu anaona kuti khamu la anthu lirikuthamangira pamodzi, anadzudzula mzimu woipawo, nanena ndi uwo, Mzimu wosalankhula ndi wogontha iwe, Ine ndikulamula iwe, turuka mwa iye, ndipo usalowenso mwa iye. (Marko 9:25)**

Musamataye nthawi yanu kumakambirana ndi ziwanda, chikuyenera kuyakhula chokha kupyolera mumau oyakhulidwa. Yesu anadzudzula ziwanda ndipo anaziuza kuti zikhale chete (Luka 4:34-35). Kumbukirani kuti mkambirano uliwonse ndiziwanda ndi wowopsya chifukwa ndi mizimu yabodza.

Mzimu Woyera azakutsogolerani kupemphero la mamasulidwe, koma ngati muli atsopano ku utumiki umenewu nde nacho chitsanzo chammene mungapempherere:

*“Mudzina la Yesu Khristu kupyolera pa ulamuliro wamphamvu Zake, Mau Ake, Mwazi ndi Mzimu Woyera...”*

*...Izi zimakhazikitsa maziko amamasulidwe...*

*“...Ndikukumanga iwe....”*

*...Yesu anati mkoyenera kumanga kaye munthu wamphamvu kenako mkumayesano kumutulutsa...*

*“...ndikukulamu iwe...”*

*... Kutumikira mamasulidwe ndi pemphero la ulamuliro, osati kunyengerera, mukhoza kuyakhula modekha, koma mukuyenera kukhala andi ulamuliro pa mphamvu zoipa mu dzina la Yesu. Yang’anani mmaso mwa munthu yemwe mukuyakhula naye.*

*“...mzimu wa \_\_\_\_\_” kapena “...iwe mzimu woyipa wa satana...”*

*“...Tulukani...”*

*...Iyi ndindomeko yotulutsa...*

*“...Popanda kuvulaza \_\_\_\_\_ (dzina la munthu litha kumasulidwa), kapena wina aliyense mnyumba mwake, ndipopanda kupangaphokoso kapena chisokonezo”*

*...Nthawi zina ziwanda zimayesera kumuvulazi munthu kapena kupanga chisokonezo.*

*“Ndikukukanizo iwe kuti usaloweso munthuyu...”*

*...Kumbukirani kuti Yesu anagwiritsa ntchito kulamula kumeneku...*

*...Ndipo ndikumasula Mzimu Woyera kuti adzde munthu uyu ndikumuyeretsa, mphamvu yomasula ya mwazi wa Yesu.”*

*...Tinauzodwa kumasula komaso kumanga. Ngati mwazindikira mzimu wina kuti ukugwira ntchito, masulani mzimu otsutsana nawo. Mwachitsanzo, manganic mzimu wakudyada ndipo masulani mzimu wozichepetsa.*

Musayerekeze kutumiza ziwanda ku Gahena. Yesu ndi ophunzira Ake sanachite zimenezi. Tiri ndi ulamuliro okha omanga, omasula, ndikutulutsa. Pali nthawi yoyikika yachiweruzo chomaliza cha ziwanda mtsogolo. Ziwanda zinati kwa Yesu:

**...Tilinanu chanu, Yesu, Inu Mwana wa Mulungu? Kodi mwabwera kuzatizua ife NTHAWI ISAKWANE? (Mateyu 8:29)**

Pemphero la onse amene akhudzidwa ndi ziwanda likhoza kuchitika popanda kusanjika manja. Yesu anagwiritsa ntchito kusanjika manja potumikira kwa mzimayi oponderezedwa ndi mizimu yozuza pa Luka 13:11-13. Mmalu mwina, Sanasanjike manja koma mmalo mwake anangoyakhula kwa ziwanda (Luka 9:42).

## **8. Mulemekzeni Mulungu chifukwa cha yankho:**

Pemphero litsatane ndi kupereka malemekezo kwa Mulungu chifukwa chamamasulidwe. Kumbukirani pachitsanzo cha m’Baibulo pa anthu khumi akhate omwe anachiritsidwa, onse anachiritsidwa koma mmodzi yekha anabwerera kukamuyamika chifukwa chakuchiritsidwako. Kuyamika mwa chikhulupiriro osati mowoneka. Mwachita zimene Mau a Mulungu amanena kuti tichite. Khulupirirani kuti wachita zomwe analonjeza kuti azachita. Muyamikeneni Iye chifukwa cha izi.

**ZINDIKIRANI ZIZINDIKIRO ZAMAMASULIDWE:**

Pankhani yolowedwa ndi ziwanda, nthawi zina ziwanda zimatuluka mwamavuvu, monga ngati kulira, kapenaso kumugwetsa munthu pansi. Pamene ziwanda zachoka (Kaya mkulowedwa kapena kuponderezedwa), pamakhala kumva kwakumasuridwa, chimwemwe, monga ngati kuchotsedwa kwa chithu cholemera.

### **PEREKANI CHISAMALIRO CHOWATSATIRA:**

Kutsatira kumasulidwa, onse amene analowedwa ndi ziwanda akuyenera kutsogozedwa kupephero lakumvomereza, kulapa, ndi kuleka tchimo linalirilonse kapena kuleka kulumikizan ndi machitachita ena aliwonse aziwanda. Ngati munthu ali ndi zinthu zakumidima (mwachitsanzo mafano, zithumwa, zipangizo zaufiti ndizina zotero), izi zikuyenera kowonongedwa.

Kuwonjezera chisamaliro chotsatira nchofunika kwambiri kwa onse omwe amasuridwa kuziwanda. Pamene chiwanda chatulutsidwa, chimasaka nthupi lina loti chilowemo. Yesu anaphunzitsa kuti kuchoka kwa mizimu yonyasa kumasiya malo opanda kanthu. Pali kuwopsya koti chiwanda chitha kubwereranso kwamunthuyu pamodzi ndi mizimu ina yoyipitsitsa:

**Pamene pali ponse mzimu wonyansa ukaturuka mwa munthu, upyola malo opanda madzi nufunafuna mpumulo; ndipo posaupeza unena, Ndidzabwera kunyumba kwanga kumene ndinaturukako;**

**ndipo pofika, uipeza yosesa ndi yokonzeka.**

**Pomwepo, upita nutenga mizimu yina isanu ndi iwiri yoipa yoposa ndi uwu mwini; ndipo ilowa nikhalira komweko; ndipo makhalidwe otsiriza a munthu uyu aipa koposa oyambawo. (Luka 11:24-26)**

Pamene chiwanda chatulutsidwa chimasowa mtenderere chikakhala kunja kwa nthupi la munthu. kupyolera kukhala munthu la munthu ndipamene chiwanda chimatha kumalamulira moyo wa munthu kuti akakwaniritse zolinga zoipa za satana. Ichi nchifukwa chake kutulutsa ziwanda kokha sikokwana. Nyumba ya uzimu ikuyenera kudzadzidwa ndi kubadwanso mwatsopano, ndikudzadzidwaso ndi Mzimu Woyera. Kuwatsatira ndi uphungu ndi utumiki ofunikira. Cholinga nchakuti amizidwe mMau a Mulungu ndi pemphero ndikuti akhale mbali imodzi ya anthu okhulupirira.

Onse amene amasulidwa ku mphamvu ya ziwanda akuyenera kulimbikitsidwa kuti apereke umboni wawo. Yesu anamuza waziwanda waku Galasa:

**Ndipo sanamlola, koma ananena naye, Muka kwanu kwa abale ako, nuwauze zinthu zazikuru anakucitira Ambuye, ndi kuti anakucitira cifundo.**

**Ndipo anamuka nayamba kulalikira ku Dekapoli zinthu zazikuru Yesu adamcitira iye; ndipo anthu onse anazizwa. (Marko 5:19-20)**

### **CHITETEZO KU MPHAMVU YA ZIWANDA**

Pali njira zapaderadera zomwe mungazitetezere nokha kumachitachita amphamvu ya ziwanda. Chitetezo chapamwamba kwambiri ndikulandira Yesu Khristu kukhala mpulumutsi chifukwa ziwanda sizingalowe mwa okhulupirira weni weni. Ziletseni kumachimo, popeza

kupyolera mu tchimo “mapeleka mpata kwa satana.” Mapereka mwayi kwa iye oti agwiritse ntchito machitachita ake aziwanda kuti azikuponderezani,

Dzadzidwani ndi Mzimu Woyera. Mizimu ya ziwanda ndi Mzimu wa Mulungu sizingapezeke muchotengera chauzimu.

## MAFUNSO OZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi yotsogolera wosawonera.

---

---

---

---

2. Kodi ndi ziwanda zitatu ziti zomwe zimachitira chiwembu nthupi, moyo, mzimu wa munthu?

---

---

---

---

3. Kodi kufunika kwa mphatso yakuzindikira polimbana ndi mphamvu ya ziwanda mkotani?

---

---

---

---

4. Kodi zithanthauzani kunena kuti kulowedwa ndi ziwanda?

---

---

---

---

5. Kodi ndimakhalidwe anji amene angawonetsedwe ndi munthu amene wagwidwa ndi ziwanda?

---

---

---

---

6. Zikuthauza chati kunena kuti munthu akulamuliridwa ndi ziwanda?

---

---

---

---

7. Kodi ndi makhalidwe otani omwe amawonetsa munthu yemwe akulamuliridwa ndi ziwanda?

---

---

---

---

---

8. Zitanthauzansi kulowedwa ndi ziwanda?

---

---

---

---

9. Ndimakhalidwe otani amene munthu walowedwa ndi ziwanda amawonetsa?

---

---

---

---

---

10. Lembani mwachidule ndondomeko zomwe zaperekedwa mu phunziro lino zochokera mmalemba zogojetsera mphamvu ya ziwanda.

---

---

---

---

---

---

(Mayakho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

## ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Mwa ma vesi 3,774 mmabuku asanu a Uthenga Wabwino, 484 amakhudzana ndi machiritso akuthupi ndi matenda amuubongo ndi chikuukitso cha akufa. Mu Marko, ma vesi okwana 209 mwa mavesi 666 amakhudzana ndi zozizwa za Yesu. Mwa ma vesi 1,257 amakamba za ma vesi a mu Uthenga Wabwino, 484 (38.9%) amakamba zazozizwa zamachiritso. Gwiritsani ntchito ndondomeko yotsatirayi kuti muphunzire za utumiki wamachiritso wa Yesu:
  - i. Cholinga cha Yesu:
    - A. Yesu anabwera kuzayakhula Mau a Mulungu:

**...Palibe chomwe ndimachita pandekha, koma zomwe Atate Andiuza, Ndikuyakhula zinthu izi... (Yohane 8:28)**
    - B. Yesu anabwera kuzachita ntchito ndichifuniro cha Mulungu:

**Pakuti ndinatsika Kumwamba, si kuti ndicite cifuniro canga, koma cifuniro ca iye amene anandituma Ine. (Yohane 6:38)**

**Tiyenera kugwira nchito za iye wondituma Ine, pokhala pali msana; ukudza usiku pamene palibe munthu angakhoze kugwira nchito. (Yohane 9:4)**

**...Cakudya canga ndico kuti ndicite cifuniro ca iye amene anandituma Ine, ndi kutsiriza nchito yace. (Yohane 4:34)**
    - C. Panali zolinga:

**...Kukacita ici Mwana wa Mulungu adaonekera, ndiko kuti akaononge nchito za mdierekezi. (1 Yohane 3:8)**

**... nchito zomwezo ndizicita zindicitira umboni, kuti Atate anandituma Ine. (Yohane 5:36)**
    - D. Chifundo ndi chomwe chimkachititsa:

Mwachitsanzo onani Mateyu 9:36; 12:9-13; 14:14; 18:27; 20:29-34; 29:34; Marko 1:41; 3:1-5; 5:19; Luka 6:6-10; 7:12-15; 10:33; 14:1-6; ndi Yohane 11:38-44

Zina zomwe Yesu anawonetsa pochiritso zinali kukwiya, kubuma, ndi kulira. Kukhudzika komwe komabwera ndi zifundo. Zifundo zake zimakafikira ku mibado ina ndipo chifundo Chake nchosatha... Umu ndi mmene timadziwira kuti Mulungu amayakha chimodzimodzi ku matenda lero. Mapeza chifundo powonetsera ichi.

**Pakuti maso a Yehova ayang'ana uko ndi uko m'dziko lonse lapansi, kudzionetsera wamphamvu kwa iwo amene mtima wao uli wangwiro ndi Iye.**

**Mwacita copusa m'menemo; pakuti kuyambira tsopano mudzaona nkhondo. (2 Mbiri 16:9)**

E. Tchito za Yesu zomwe zinasalanga Atate:

**...cifukwa ndicita Ine rimene zimkondweretsa iye nthawi zonse. (Yohane 8:29)**

ii. Maumboni oti Yesu anachiritsa onse:

- Machitidwe 10:38
- Luka 4:40; 6:17-19
- Luka 9:11
- Mateyu 12:15
- Mateyu 4:23-25
- Mateyu 9:6,35
- Mateyu 10:1; 14:14,34-36

iii. Mau otsiriza a Yesu:

Mau Ake otsiriza anali okhudzana kutuma kukalalikira ndi kuphunzitsa Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu ndi kukawonetsera mphamvu pochilitsa ndi kutulutsa ziwanda (Marko 16:18).

iv. Matenda apaderadera omwe Yesu anachiritsa:

- Khunyu
- Kusamva ndi kusayakhula
- Kufa ziwalo
- Kuchucha kwa mwazi
- Ogwidwa ndi ziwanda
- Mkono wopuwala
- Khungu
- Zowawa
- Khutu lodulidwa
- Kudzutsa akufa mmalo atatu osiyana
- Kubwezeretsa (Marko 9:43, imawonetsera mwachindunji kusowa kwa nthiti—chozizwa cholenga)

v. Njira zomwe anagwiritsa ntchito:

A. Nthawi zina Yesu amkayitana wodwaloyo kwa Iye yenkha: Marko 3:1-6

B. Nthawi zina, anthu amkamuyitana Yesu:

1. Watchito wa Kenturiyo: Mateyu 8:5-13; Luka 7:1-10
2. Mwana wa mkazi wa Yayero: Mateyu 9:18-19; 23-26

C. Amkathana ndi munthu yense:



1. Kukhululukira tchimo pamodzi ndi kuchiritsa.
2. Anthu amkatha kuvomereza mosavuta machiritso akuthupi kusiyana ndi kuyeretsedwa: Luka 8:26-39
3. Nthawi zina amayamba kaye wachiritsa, kenako mkukhululukirano tchimo: Luka 17:9; Yohane 5:14
4. Nthawi zina amkayamba kaye kukhululukira tchimo, kenako mkuchiritsa: Marko 2:1-12

D. Nthawi zina machiritso amkatha kuchitika popanda chikhulupiriro chamunthu wodwalayo (Koma izi sizinanenedwe):

- Lazaro: Yohane 11:1-44
- Khutu la kapolo wawamsembe: Luka 22:50-51
- Wogwidwa ndi mzimu winyasa ku Garasa: Marko 5:1-20
- Munthu wosava ndi kusayakhula: Marko 7:32-35
- Kuchiritsidwa kwa mpongozi wa Simoni Petro: Luka 4:38-39
- Kuukitsidwa kwa mnyamata ku Nayini: Luka 7:12-15
- Munthu wa dzanja lopuwala: Marko 3:1-5
- Munthu wosawona chibadwire: Yohane 9:1-7
- Mwana wamkazi wa Abrahamu: Luka 13:10-13
- Mwana wa mkuru: Yohane 4:46-50
- Kapolo wa Kenturiyo: Mateyu 8:5-13
- Mwana wamkazi waku Kanani: Mateyu 8:5-13
- Mwana wa Yairo: Marko 5:35-43

E. Nthawi zina machiritso amkachitika chifukwa chachikhulupiriro kwa munthuyu:

- Akhungu awiri: Mateyu 9:27-31
- Wakhate: Mateyu 8:2-4; 20:29-34; Marko 1:40-44
- Akhate khumi: Luka 17:11-19
- Amuna awiri akhungu: Mateyu 20:29-34
- Batumeyo wakhungu: Marko 10:46-52; Luka 18:35-43
- Mkazi odwala nthenda ya mwazi: Mateyu 9:20-22; Marko 5:25-34; Luka 8:43-48

F. Amkagwiritsa ntchito mau osiyasiyana:

1. Nthawi zina amkangoyakhula Mau okha basi:
  - Mwana wa Abrahamu: Luka 13:10-13
  - Mwana wa mkuru: Yohane 4:46-52
  - Batumeyo wakhungu: Marko 10:46-52
  - Amuna awiri akhungu: Mateyu 9:27-31
  - Kapolo wa Kenturiyo: Mateyu 8:5-13
2. Nthawi zina amkayakhula mau olamula:
  - Munthu wamanjenje: Luka 5:22-24,

- Mwana wa Yayiro: Marko 35-43 5:17-26
3. Amkaphatikiza kulamula ndi kukhudza:
    - Wakhate: Mateyu 8:2-4
    - Amuna awiri akhungu: Mateyu 9:27-31
    - Mpongozi wa Simoni Petro: Luka 4:38-39
    - Munthu wosamva ndi kusalakhula: Luka 7:32-35
    - Mwana wa mkazi wamasiye: Luka 7:12-15
  4. Amkapemphera:
    - Mpongozi wa Simoni Petro: Luka 4:38-39
    - Munthu wosamva ndikusalakhula: Marko 7:32-35
    - Mwana wa mkazi wamasiye: Luka 7:12-15
    - Lazalo: Yohane 11:38-44
    - Munthu wa dzanja lopuwala: Marko 3:1-5
- G. Kuwonjezeraso kukhudzana, Amkachiza kuchokera patali:
- Kapolo wa Kenturiyo: Mateyu 8:5-13
  - Mwana wa mkuru: Yohane 4:26-50
  - Mwana wamkazi waku Kanani: Mateyu 15:21-28
- H. Nthawi zambiri amkakonda kulamula odwala kuti achite chinachake monga ngati mbali imodzi yanjira yamachiritso:
1. Munthu wa dzanja lopuwala: Tambasula dzanja lako: Luka6:6-11
  2. Munthu wopuwala pa thamando la Betesda: Tauka, yalula mphasa yako, nuyende: Yohane 5:1-9
  3. Mkuru ndi mwana wake wadwala: Muka... Yohane 4:46-54
  4. Wakhate: kaziwonetsere kwa wamsembe: Luka 17:11-19
  5. Wakhungu: Muka, kasambe m'nthamanda la Siloamu: Yohane 9:7
- I. Amkatumikira machiritso pawonekera (Pgulu, Sunagoge) ndi mseri (makomo, kwamutnhu)
- J. Amkagwiritsa ntchito zinthu zonyozeka:
1. Malovu
  2. Thope
  3. Zala makutu
  4. Mphonje ya chovala Chake
  5. Kusamba mmadzi
- K. Nthawi zina wodwala amkamukhudza Iye:
- Marko 5:23-24
  - Luka 6:17-19
  - Marko 3:10
  - Marko 6:56

L. Nthawi zina amkawakhudza wodwala:

1. Amuna awiri akhungu: Mateyu 9:27-31
2. Anthu anthenda zosiyanasiyana: Luka 4:40
3. Wakhate: Luka 5:13
4. Mkazi wopeteka: Luka 13:10-13

M. Kutsatira malangizo kunali kosiyana. Mwachitsanzo mpongozi wa Petro anamuka pakamama pake mkuyamba kutumikira kwa omwe anali mnyumbamo. Yesu anayitana mwana wa Yayiro kuti atumikire pogawa chakudya chomwe wapatsidwa.

N. Machiritso a Yesu amkachitika mu:

- Panyumba (Pakhomo peni peni, mkati)
- Pamisokhano yapanja: Mizinda, panthamado, mapiri, mungalawa
- Pamene mwambo wamaliro ukuchitika
- Pamanda amunthu wakufa
- Mkachisi
- Kumanda
- Nthawi yakudya
- Panjira popita ku mzinda wina
- Mmunda

O. Panali kuyakha kosiyasiyana ku zozizwa ndi machiritso:

- Kunyadira
- Kuwopa Mulungu
- Kudabwitsika
- Kukanidwa ndi banja komaso atsogolero achipembedzo
- Ziwanda kulira
- Mkwiyoy
- Kutchuka
- Kukweza Mulungu
- Kufunsa mafuso (zonse zonedwa ndi phekesera)
- Chipulumutso chabanja lonse

Gwiritsani ntchito ndondomeko zotsatirazi kuti mudziwe mwatsatanetsane zamachiritso omwe anachita Yesu:

### **Machiritso a munthu pa yekha**

#### **Machitachita a ziwanda omwe ananedwa mwapaderadera**

- Mkazi wolumala: Luka 13:10-17
- Munthu wa mzimu wonyasa Msunagoge: Marko 1:23-28; Luka 4:31-37

- Munthu waku Galasa wogwidwa ndi mizimu yoyipa: Mateyu 8:28-32; Marko 5:1-13; Luka 8:26-33
- Mkazi wanthenda ya mwazi: Mateyu 9:20; Marko 5:25-34; Luka 8:43-48
- Mwana wa mkazi wa ku Kanani: Mateyu 15:21-28; Marko 7:24-30
- Mwana wamzimu woyipa: Mateyu 17:14-21; Marko 9:14-29; Luka 9:37-45
- Chiwanda chosayakhula: Mateyu 9:32-33
- Chiwanda chakhundu ndi chosayakhula: Mateyu 12:22-30; Marko 3:22-27; Luka 11:14-26

### **Machiritso amunthu payekha: Machitachita aziwanda sanatchulidwe**

- Mpongozi wa Petro: Mateyu 8:14-15; Marko 1:30-31; Luka 4:38-39
- Wakhate: Mateyu 8:2-4; Marko 1:40-42; Luka 5:12-13
- Wamanjenje: Mateyu 9:1-8,35; Marko 2:10-12; Luka 5:17-26
- Munthu wadzanja lolumala: Mateyu 12: 9-13; Marko 3:1-5; Luka 6:6-11
- Mwana wa Yayero: Mateyu 9:18-19; 23-26; Marko 5:22-24, 35-42; Luka 8:41-42, 49-56
- Munthu wakhungu pa Betisda: Marko 8:22-26
- Munthu wobwadwa wakhungu: Yohane 9:1-14
- Mkazi wogwidwa chigololo Yohane 8: 1-11

### **Kuchiritsidwa kwa gulu la anthu**

- Wakhundu ndi wopuwala mkachisi: Mateyu 21:14
- Ziwanda zambiri: Marko 1:39
- Gulu ku Galireya: Mateyu 4:23-24; Marko
- Anthu osiyanasiyana: Luka13:52
- Anthu ochuluka: Mateyu 9:35; 12:15-21; Marko 3:10-11
- Asanadyetse anthu okwana 5,000: Mateyu 14:13-14; Luka 7:18-23
- Asanadyetse anthu 4,000: Mateyu 15:29-31
- Khamu ku Yolodani: Mateyu 19:1-2
- Munthu wakhungu mkachisi: Mateyu 21:14
- Odwala ena ku Nazarete: Mateyu 13:53-58; Marko 6:1-6

3. Phunzirani zambiri zokhudzana machiritso ndi mamasuridwe pophunzira utumiki wa ophunzira:

### **Ophunzira analamuliridwa komaso anatumidwa ndi Yesu kuutumiki wamachiritso.**

	<b>Mateyu</b>	<b>Marko</b>	<b>Luka</b>
<b>Machitidwe</b>			
Kutumidwa kwa 12	10:1-42	6:7-13	10:1-6

Kutumidwa kwa 70

Mphamvu yomanga/kumasula 16:17-19

Kutuma komaliza 28:16-20 16:14-20 24:44-53  
1:1-11

**Analepherepo:** Mateyu 17:14-21; Marko 9:14; Luka 9:37-45

**Anakumana ndi kucedweretsedwa kwa machiritso:** Epafrodito (Afilipi 2:25-30); Timoteo (1 Timoteo 5:23); Tropiyasi (2 Akorinto 8:18-22)

**Ophunzira anakwanitsa kuthana ndi mavuto ofanana ndi amene Yesu anachiritsa:**

<b>Chochitika Paulo</b>	<b>Zochita za Petro</b>	<b>Zochita za</b>
Kuchiza wopunduka	Pakhomo Machitidwe 3:1	Ku Lustra Machitidwe 14:8
Kuchiza odwala Machitidwe 28:7	Eneya: Aanadwa kwa  Zaka 8: Machitidwe 9:12	Kuchizidwa kwa Popiyo:
Zinthu zosazolowereka Pochiritsa	chithunzinthuzi Machitidwe 5:12	Kansalu kamanja Machitidwe
Khamu lichizidwa	Machitidwe 5:16	Machitidwe 28:9
Kuukitsidwa kwa akufa	Machitidwe 9:36	Machitidwe 20:7

**Anathananso ndi mavuto awa:**

Nthenga ya malungo ndi kamwazi	atate wake a Popiyo	Machitidwe 28:8
Khungu	Paulo	Machitidwe 9:8
Kumvulala kwa mmutu (kufa)	Utiko	Machitidwe 20:9
Kudwalika, choyambitsa chosadziwika	Tabita	Machitidwe 9:37
Manjenje	Eneya	Machitidwe 9:33
Kupuwala	opuwala ochuluka	Machitidwe 8:7; 3:2; 14:8
Ogwidwa ndi ziwanda	Filipo	Machitidwe 16:16-40
Kulumidwa ndi njoka	Paulo	Machitidwe 28:3-6

**Panalibe njira yokhazizika yamachiritso. Anagwiritsa ntchito:**

- Kusanika manja: Machitidwe 5:12; 14:3; 19:11; 28:8
- Mau mophatikizana ndikusanjika manja: Munthu wopuwala (Machitidwe 3:1-10); Maso a Paulo (Machitidwe 9:17-19)
- Kuyakhula mau (kulamula ndi ulamuliro): namwali wa mzimu wambwebwe (Machitidwe 16:18); wopuwala ku Lustra (Machitidwe 14:10)
- Pemphero: Maso a Paulo (Machitidwe 9:36-43); atate wake a Popiyo (Machitidwe 28:8-9)
- Kasalu kopempherera: Machitidwe 19:11-12
- Chithunzithuzi: Machitidwe 5:12-16
- Tinsalu tamanja: Machitidwe 19:12
- Zonzungulira: Machitidwe 14:19-20
- Popanda ndi njira komwe...kupitirira kwa chitetezo: Machitidwe 14:19-20
- Mau ndi kulamuliridwa kuchitapo kanthu: Eneya (Machitidwe 9:33-34); munthu wopuwala (Machitidwe 3)

**Machiritso apagulu mu buku la Machitidwe**

- Zizindikiro ndi zozizwitsa zochuluka: 2:42-47
- Pemphero la kulimbika ndi zizindikiro zamachiritso: 4:23-31
- Amabiri anachiritsidwa ku Yerusalemu: 5:12-16
- Sitifano anachita zozizwitsa zochuluka: 6:8-15
- Filipo anachiritsa anthu ochuluka ku Samaliya: 6:5-8
- Paulo ndi Banaba achita zozizwa: 14:3
- Paulo achiritsa odwala ku Aefeso: 19:11-12
- Odwala achiritsidwa ku Mata: 28:8-9

## CHIYAMBI CHA GAWO LACHITATU

### “Pamene Muli Kumeneke”

Gawo iyi la “Chotupisa-ngati uvageli” lakhazikika pa ndondomeko zomwe zinawonetseredwa mu Mpingo wa Chipangano Chatsopano pazomwe mukuyenera kuchita pamene muli kumene. Izi zimaonetsera kuti uvangeli sukhala wa thunthu pokhapokha mutankhazikitsa mpingo pakati pa okhulupirira atsopano.

Malo aliwonse amene uvangeli wa Chipangano Chatsopano umachitika, kumakhazikitsidwa mpingo. Atumwi anakhazikitsa mpingo watsopano pamene anali kumeneke asananyamuke kupita mudzi wina kukalalikira. “Kukhazikitsa Mpingo” mawu awa agwiritsidwa pokamba njira yomwe mungayambire mpingo watsopano. Mawu awa agwiritsidwa ntchito chifukwa wina akabzala mpingo watsopano monga momwe mulimi abzalira mbeu kumunda. Munthaka ya chonde, mbeu ikabereka mbeu ina yonga inadzalidwa ija.

Mau oti “kubzala” amanenedwa chifukwa sichinthu chabwino kupanga mpingo omwe sukugwiridzana ndi chikhalidwe cha anthu amuderalo. Sichabwino kuyika mpingo kenako ndikuutsiya kuti udzivutika. Ukuenera kukhazikitsidwa, kutathaunza kuti midzu ikalowe pansu, ukakule, ndipo ukapitiridze kuchita chita muuzimu.

Kulalikira kosakhazikitsa mipingo ma dera zili ngati kubereka ana koma kumakana kutenda udindo owasamalira ngati kholo. Munthu asanenedwe kuti walalikiridwa kufikira atakhala mbali ya mpingo wina muderalo. Kutu mukakwaniritse izi, pakuenera kuti pakhale mpingo wamudera. Malowo asanenedwe kuti alalikiridwa kufikira mpingo utakhazikitsidwa.

Mu gawo ili mukaphunzira chitsanzo cha Chipangano Chatsopano cha mpingo ndipo mukaphunzira ndondomeko za momwe mungakhazikitsire mpingo, kukudza ndikuwutukula. Phunziro lamu The Harvestime International Institute lakhazikika pa njira zosiyana siyani zokhazitsira mpingo. Kutu mukaphunzire zambiri mukuenera kupedza mabukhu awa:

**Njira zochulukitsira:** limafotokodza mene mungachulukitsire zinthu zauziu ndi kukudza mpingo watsopano mu madera odzungulira, kukulitsa, kuchulukitsa ndi kubweredza kukula.

**Njira za baibulo zogwirira ntchito:** zikutsogolerani mene mungatsakhire komanso kutukula adzitsogoleri ampingo.

**Kuwunikira dera:** zikuthandizirani kudziwa mene dera lingalandirire Uthenga Wabwino ndikukodzekera kulalikira ndi kubzala mpingo.

**Kuchita ndi zolinga:** zikuphunitsani kudziwa cholinga cha kumano wamu dera, dongosolo, ndikupanga mpingo.

**njira zobweretsa anthu:** zikuthandizirani mene mungabweretsere ma membala onse pamodzi, ndikuwatsimikidzira kuti akatumikire monga mwa mphatso zawo za Uzimu.

**Leaven-Like Evangelism:** umanena kuti kukhazikitsa mpingo ndi cholinga chomalidza cha kulalikira.

## CHAPUTALA 20

### KUBZALA MPINGO: CHITSANZO

#### ZOLINGA:

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba vesi yapa mtima
- Kunena mawu oti “mpingo”.
- Nenani mutu wa mpingo.
- Nenani thupi la mpingo.
- Nenani atsogoleri a mpingo.
- Fotokodzani cholinga cha mpingo.
- Nenani chitsadzo cha Chipangano Chatsopano.

#### VESI YAPA MTIMA:

**Kotere kuti munayamba kukhala inu citsanzo kwa onse akukhulupira m’Makedoniya ndi m’Akaya. Pakuti kuturuka kwa inu, kudamveka mau a Ambuye, osati m’Makedoniya ndi Akaya mokha, komatu m’ malo monse cikhulupiriro canu ca kwa Mulungu cidaturuka; kotero kuti sikufunika kwa ife kulankhula kanthu. (1 Atesalonika 2:7-8)**

#### ZAMKATIMU

Lamulo la Yesu linali lopita kumayiko wonse ndi Uthenga Wabwino, kuyambira mu Yerusalemu ndi Yudeya ndikufikira ku Samariya ndi mayiko onse adziko lapansi. Yesu analamulaso “Pamene mukupita chilisani odwala, chosani ziwanda...”

Koma kuwonjedzera pama udindo awiriwa, tapeza njira yachitatu yomwe ikukambidwa mu Chipangano Chatsopano. Kulikonse okhulupirira amapita, pamene anali kumeneko amabzala mipingo imene imakaphunzitsa otembenuka atsopano kuti akakule muuzimu. Iyi ndi phunziro loyamba pamaphunziro atatu amene mungadzalire mipingo. Chaputala ichi chikukhudza za Chipangano Chatsopano ngati chitsanzo chomwe mungaphunzirire pakuyambitsa mpingo. Phunziro lina likakamba za njira ya Baibulo pobzala mpingo, Chaputala 22 chikufotokodza mene mpingo umakulira.

#### CHITSANZO CHA CHIPANGANO CHATSOPANO

“Chitsanzo” ndi chitsanzo chomwe chaperekedwa kuti chikatsatiridwe. Mbiri ya mpingo woyamba mu nthawi ya Chipangano Chatsopano inasungidwa kuti ikapereke chitsanzo pa momwe mungabzalire mipingo yatsopano.

#### TANTHAUDZO LA MPINGO:

Mawu oti “mpingo” akutanthaudza “kukumana kwa anthu amene ali a Ambuye” kapena “anthu amene ayitanidwa.” Mpingo wachowonadi sichinyumba kapena bungwe. Ndi okhulupirira onse obadwa mwatsopano, anthu amene ayitanidwa “Mwala wamadziko” mu 1



Petro 1:5. Mawu oti “mpingo” agwiritsidwa kunkumano wa anthu amene ali gawo lalikulu, Thupi lonse la Khristu.

### **MUTU WA MPINGO:**

Yesu ndiye mutu wa mpingo. Mulungu anati ndipo...

**...anakanza zonse pansu pa mapazi ace, nampatsa Iye akhale Mutu pamtupa zonse,**

**Kwa Eklesia amene ali thupi lace, mdzazidwe wa Iye amene adzaza zonse m'zonse. (Aefeso 1:22-23)**

Mpingo unakhazikitsidwa pa nthanthwe Yesu Khristu ndi pamadziko a “mwala wapangodya” umune ukakhadzikitsidwa ndi atumwi ndi aneneri oyamba.

### **THUPI LA MPINGU:**

Okhulupirira onse obadwa mwatsopano ndi mbali ya Thupi la Khristu. Ndife anthu amene Mulungu amakwaniritsa ntchito yake pa dziko lapansi. Mpingo wafotokodzedwa ngati thupi chifukwa limachita chita monga momwe lichitira thupi la munthu. Membala aliyense ali ndi mphatso ya uzimu ku utumiki ndicholinga cheni cheni muma dongosolo la Mulungu, monga mene chiwalo cha munthu chiri ndikuchita kodabwitsa (1 Akolinto 12).

Thupi la munthu ndichitsanzo chimodzi mwadzambiri zamu Chipangano Chatsopano chimene chimagwira ntchito pofotokodza mpingo. “Chithunzithunzi” ndimawu amene amagwiritsa ntchito chinthu chimodzi pofotokodza chinthu china. Onani “Maphunziro owonjedzera” gawo la phunziro ili pakuonjedzera chinthunzi nthunzi chamu Chipangano Chatsopano chomwe chikufotokoza za mpingo.

### **ADZITSOGOLERI A MPINGO:**

Mulungu anayika adzitsogoleri ndi mphatso zosiyanasiyana mu mpingo. Izi zikuphatikidza, Atumwi, Aneneri, Alalikiri, Azibusa, ndi Aphunzitsi (Aefeso 4:11-16). Cholinga ndichoti akonzere oyera mtima kuntchito ya utumiki. Amachita ichi powanthandidza kuti akadzindikire ndikugwiritsa ntchito mphatso zawo za uzimu. Akulu a mpingo ndi azitumiki nawotso amatandizira ku ntchito ya mpingo muntchito zowoneka ndi maso za utumiki. Onani Tito 1 ndi 1 Timoteo 3.

### **CHOLINGA CHA MPINGO:**

Cholinga cha mpingo ndikukwaniritsa chokhumba cha Mulungu ndi dongosolo lake mene afotokodzera mu Aefeso 1:9-11 ndi 3:10-11. Chipangano Chatsopano chimakamba kuti ntchito zonse za mpingo zinayikidwa madera awiri:

-Choyamba unali uvangeli: Ophunzira anali okangalika ndikulaikira ndikuphunzitsa Uthenga Wabwino, kubatidza otembenuka mtima kumene, kuwatsogoleri ku ubatidzo wa Mzimu Oyera, kuchiritsa odwala, kumasula ndikuchotsa ziwanda.

-Chachiwiri kuyeretsa: Kuyeretsa ndikutanthauza kuti kuwumba. Okhulupirira anabzala mipingo kuti akaphunzitse komanso kuyendetsa otembenuka atsopano kufikira ata kwima muuzimu ngati ophunzira.

Pali ndondomeko 6 zomwe zikupedzeka mu cholinga cha mpingo wa Chipangano Chatsopano:

**Choyamba:** amatenga udindo wotenga Uthenga Wabwino kumadera komwe amakhala, dziko lakwawo ndi dziko lonse lapansi. Mpingo unapereka Yesu ku Dziko lapansi ngati Ambuye ndi Mpulumutsi. Anatsogolera anthu ku ubale wabwino ndi Yesu kuti akayende mu chipulumutso komanso moyo watsopano.

**Chachiwiri.** Uthenga Wabwino unalalikiridwa kwa anthu osakhulupirira kwa amene anali kumeneko. Atumwi sanalipire holo kapena kupangitsa tsokhano manyumba akulu akulau. Amakumana mu kachisi, manyumba mwawo kapena chipanda chapamwamba (Macitidwe 2:46 ndi 5:42). Analalikira muchitsitsimutso hachikulu komanso kwa munthu modzi modzi.

**Chachitatu:** Uthenga Wabwino unalalikiridwa ngati chipulumutso kudzera mwa Yesu, osati zachipembedzo kapena zochitika dzina. Zimakhala zamu Baibulo basi, Zokhudzana ndi Khristu, zosowa komanso kuwonetsera mphamvu ya Mulungu.

**Chachinayi:** Uthenga umapita kwa akulu akulu chifukwa akulu akulu akatembenuka mtima ndiye kuti ana awoso atembenukansa. Munjira iyi ndiye kuti mabanja awoso akhala okhulupirira. (Werengani khani ya konoliyasi mu Macitidwe 10; Mdindo waku filipi mu Macitidwe 16:31-15; Sitefano mu 1 akolinto 1:16; Onesimus mu 2 Timoteo 1:16 ndi Filimoni in Filimoni 2).

**Chachisanu:** Okhulupirira amaperekedwa ku moyo wa mpingo kumadera awo. Amaphunzitsidwa ndi kuyang'aniridwa muma pephero ndi mikumana ya uzimu ndi mamembala ena a thupi la Kristu (Macitidwe 2:42). Okhulupirira amakhazikitsidwa muziphunzitso, malamulo ndi zochita za moyo wachi Kristu. Amaphunzitsidwa kuti “akasunge zonse” zomwe Yesu anawaphunzitsa.

**Chinsanu chimodzi:** Mpingo umasankha ndikutumidza anthu omwe ayitanidwa kuti akalalikire za Uthenga Wabwino kumadera ena (Macitidwe a Atumwi 13:1-3).

## CHITSANZO CHAKU ATESALONIKA

Mpingo waku Atesalonika umapereka chitsanzo cha utumiki ndikuyeresera ichi chinali chidzindikiro cha mipongo yamu Chipangano Chatsopano. Paulo anawaremba kuti...

**Kuti Uthenga Wabwino wathu sunadza kwa inu m'mau mokha, komatunso mumphamvu, ndi mwa Mzimu Woyera, ndi m'kucuruka; monga mudziwa tinakhala onga otani mwa inu.**

**Ndipo munayamba kukhala akutsanza anthu, ndi a Ambuye m'mene mudalandira mauwo m'cisautso cambiri, ndi cimwemwe ca Mzimu Woyera;**

**Kotero kuti munayamba kukhala inu citsanzo kwa onse akukhulupirira m'Makedoniya ndi m'Akaya.**

**Pakuti kuturuka kwa inu, kudamveka mau a Ambuye, osati m'Makedoniya ndi Akaya mokha, komatu m'malo monse cikhulupiriro canu ca kwa Mulungu cidaturuka; kotero kuti sikufunika kwa ife kulankhula kanthu.**

**Pakuti iwo okha alalikira za ife, malowedwe anthu a kwa inu anali otani; ndi kuti munatembenukira kwa Mulungu posiyana nao mafano, kutumikira Mulungu weni weni wamoyo,**

**Ndi kulindiriri Mwana wache acokere Kumwamba, amene anamuukitsa kwa akufa, Yesu, wotipulumutsa ife ku mkwiyo ulinkudza. (1 Atesalonika 1:5-10)**

Onetsetsani posatira ndondomeki mugawo iyi:

**“UTHENGA WATHU WABWINO UNABWERA KWA INU”**

Uthenga unabwera kwa anthu aku Atesalonika ndi Mawu a Mulungu ndikuwonetseredwa mphamvu ya Mulungu. Inalakhulidwa pakukhuzidwa mtima ndi mphamvu ya Mzimu Woyera.

**“MUNALANDIRA MAWU”**

Panali kulingalira kosusana ku Uthenga Wabwino, pakuti anthu awa analandira mkati mwakuva zowawa zambiri. Analandira uthenga ndichimwemwe cha Mzimu Woyera.

**“MUNAKHALA OTSATIRA”**

Otembenuka mtima anatsatira ziphunzitso ndi chitsanzo cha Yesu ndi atumwi.

**“MUNAKHALA CHITSANZO KWA OPHUNZIRA ONSE”**

Munasatira chitsanzo, kenako munakhala chitsanzochi.

**“MAWU A AMBUYE ANAYAKHULIDWA KUCHOKERA KWA INU”**

Anthu awa analibe nyumba zowulutsa mawu, zakanema, zoonera kapena zovera, kapena zolengedzetsa zomwe timagwiritsa pano. Anagwiritsa njira ya baibulo ya kukumana ndi modzi modzi kugawana Uthenga Wabwino.

## MAFUNSO OZIYESA NOKHA

1. Lembani verse yapa mtima.

---

---

---

2. Fotokodzani mawu oti “mpingo”

---

---

---

3. Mutu wa mpingo ndindani?

---

---

---

4. Thupi la mpingo ndindani?

---

---

---

5. Kodi adzitsogoleri ampingo omwe mulungu anatumidza ndi ati?

---

---

---

6. Kodi cholinga cha mpingo ndichani?

---

---

---

7. Kodi chitsanzo chanji cha Chipangano chatsopano chomwe chakambidwa mu phunziroyi?

---

---

---

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

## ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Werengani bukhu la Macitidwe a Atumwi ndi makalata amu Chipangano Chatsopano. Werengani palipose pomwe mawu oti mpingo akunenedwa. Chongani mawu amenewo “KU” kulalikira ndi “YE” kuyeretsedwa. Pakuwerenga kwanu mukawona mene mpingo oyamba unakwaniritsira zithu ziwiri izi za cholinga cha uzimu.
2. Izi ndi zinthuzi nthuzi zina zomwe zikukamba za mpingo:

-Banja la Ambuye: Mateyu 6:9; Luka 11:2; Aroma 8:15; Ahebri 2:10-11; Aefeso 3:14-15; Aroma 8:17; 1 Timoteo 3:15

-Chiyanjano cha Okhulupirira: 1 Yohane 1:3; Macitidwe 2:42-44 Gulu lawothamanga: 1 akolinto 9:24-26; Agalantiya 2:2; 5:7; Afilipi 2:16, 2 Timoteo 2:5; 4:7; Ahebri 12:1; 1 Timoteo 6:12

-Atsirikali a Ambuye: 2 Akolinto 10:4-5; Aefeso 6:11-12; 1 Timoteo 1:18; 2 Timoteo 2:3-4; 1 Akolinto 9:7; 1 Petro 2:11

-Nkhonsa: Macitidwe a Atumwi 20:28; 1 Petro 5:2-4

-Sukulu: (Chiganidzo choti mpingo ndi sukulu zikuonetsera pa fundo za kuphunzitsa kumachitika ngati mbali ya utumiki) Mateyu 28:18-20

-Kapolo: (Wa Uthenga Wabwino) Mateyu 25:14-30; 1 Akolinto 4:1-2; Aefeso 4:12

-Chomanga: 1 Akolinto 3:9-15; Aefeso 2:20-22; Mateyu 16:18; 21:42; 1 Petro 2:4-7, Luka 6:46-49; Macitidwe 4:11; Aroma 15:20; Masalmo 118:22

Chitsitsi: Aefeso 3:4-6

-Munda: 1 Akolinto 3:6-9; 2 Timoteo 2:6; Mateyu 13:3-8, 18-20.

-Ansembe achifumu: 1 Petro 2:5-9

-Mkwati wa Kristu: Yohane 3:29; 1 Akolinto 11:2; Aefeso 5:21-32; Cibvumbulutso 19:7-9

-Mtumiki m'malo mwa Kristu: Aefeso 6:20; 2 Akolinto 5:20

-Mzati ndi mchirikidzo wa choonadi: 1 Timoteo 3:15

-Nyumba ya Ambuye: Acts 17:24; 1 Akolinto 3:15-17; Aefeso 2:21-22; 1 Peter 2:4-5

-Okhulupirira: Afilipi 3:20; Aroma 12:2; Ahebri 11:3

-Njira: Macitidwe a Atumwi 9:2; Yohane 14:6

-Cholowa chake: Aefeso 1:18

-Antchito ake: Aefeso 2:10; 1 Yohane 5:14

-Kuuna kwa dziko lapansi: Mateyu 5:14-16; Aefeso 5:14

-Mchere wa dziko lapansi: Mateyu 9:49-50; Luka 14:14

-Atsodzi a Anthu: Marko 1:17; Mateyu 4:18-20; 13:47

-Mayesero akanthawi kochepe: 1 Petro 1:6-7; 4:12-17; Yakobo 1:3

-Inu ndinu nthambi: (Achikunja kuyikidwa kuthipi Lake): Aroma 11:16-24

## CHAPUTALA 21

### KUBZALA MPINGO: NJIRA ZOYENERA

#### ZOLINGA:

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Lembani vesi yapa mtima.
- Nenani njiri zozalira mpingo zobweredza.
- Nenani zolinga 7 za utumiki umene Paulo analunjika pa ntchito ya kulalikira.

#### VESI YAPA MTIMA:

**Kwa Iye ukhale ulemerero mu Mpingo ndi mwa Kristu Yesu, kufikira mibadwo yonse ya nthawi za nthawi. (Aefeso 3:21)**

#### CHIYAMBI

Muphunziro ili mukaphunzira mene uvangeli umakutsogolererani kukabzala mipingo pamene ma membala ake amaphunzitsidwa kuti nawonso akachite monga mwachitira inu. Pakutsatira ndondomeko iyi, kubzala mpingo kumakhala kwa mphamvu, mphamvu yopitiridza ya kutumikira.

Kuwonjedzera kuphunzira za kubzala mpingo kodzungulira, “Zoonjezera Pophunzira” gawo ili zapereka mfundo zomwe mungatsatire pofuna kubzala mpingo watsopano.

#### NJIRA ZODZUNGULIRA ZOBZALIRA MPINGO

Utumiki wa Paulo umapereka chitsanzo chabwino cha kubzala mpingo munthawi ya Chipangano Chatsopano. Khalani ndikutsimikidzika powerenga baibulo lanu:

Izi ndinjira zozungulira pobzala mpingo mu Chipangano Chotsopano zomwe zingawiritsidwe ntchito nthawi ya makono ano:

#### 1. OGWIRA NTCHITO KUTUMIZIDWA: Macitidwe a Atumwi 13:1-4; 15:39-40

Ogwira ntchito amaphunzitsidwa ndikutumidzidwa kuti akafikire m'madera ndi Uthenga Wabwino. Okhulupirira apa mpingo amathandiza kukodzekera, kutumidza, kuthandiza, ndikuthandiza onse omwe Mulungu wawapatula kuntchito yake.

#### 2. ANTHU KUFIKIRIDWA: Macitidwe a Atumwi 13:14-16; 14:1; 16:13-15

Pamene walowa mdera latsopano, Paulo amafikira adzitsogoleri amipingo yomwe inali kale. Amafuna kupedza kuvetsetsana ndi chithandizo kuchokera kwa atsogoleri ngati kunali kotheka. Nkhamu ndi munthu modzimodzi amafikiridwa, cholinga chinali chopedza anthu ambiri overa Uthenga Wabwino ngati kuli kotheka.

#### 3. UTHENGA WABWINO KUPEREKEDWA: Macitidwe a Atumwi 13:17; 16:31

Uthenga wabwino umaperekedwa polalikira, kuphunzitsa, kuyikira umboni, ni kuwonetsera mphamvu. Njira zosiyana siyana zimagiwiritsidwa ntchito kuti Uthenga Wabwino uperekedwa moveka bwino. Njira yomwe imagwira nthito mizinda inali yolalikira mumakachisi (Macitidwe a Atumwi 14:1). Kwina, anthu oyenera amagawidwa ma gulu

apadera dera (Macitidwe 19:9). Kutumikira kwapa dera dera kumachita kwa munthu modzi modzi kumachitika madera ena ndi chilankhulo ngakhaleso njira zimtsidwa kuti akapereke Uthenga Wabwino moyenera (Macitidwe a Atumwi 22:2).

#### **4. KUTEMBENUKA MTIMA KWA AKUMVERA: Macitidwe 13:48; 16:14-15**

Kupereka Uthenga Wabwino mochimika kumabweretsa kusithika, anthu kulandira uthenga wachipulumutso ndi kulapa machimo.

#### **5. KUTSOKHANA KWA OKHULUPIRIRA: Macitidwe 13:43**

Paulo tsanasiye kulalikira ndikusitha anthu. Amatsokhanitsa okhulupirira ku mpingo wamudera. Okhulupirira amawonetsedwa mwachangu ku chiyanjano ndi kukhala odekha ku thupi la Kristu. Nthawi ndi malo zimakhazikitsidwa kuti azibwera pamodzi mu mpingo atsopano.

#### **6. KUSIMIKIDZIKA KWA CHINKHULUPIRIRO: Macitidwe 14:21,22; 15:41**

Ngati mene zanenedwera ndi ntchito yayikulu (Mateyu 28:19-20), maphunziro ena amabwera pakutha pakutembenuka mtima. Chiphunzitsi ichi, zimaphunzitsidwa pakati pa mpingo yamudera, okhulupirira amakhazikitsidwa pamene amaphunzira ndondomeko ya chikhulupiriro cha akristu ndimomwe angakhaliye mu Ufumu wa Mulungu. Kutsimikizika kwa chikhulupiriro kumakudza kukula muuzimu ndikuthandidzira okhulupirira kukaziwa mphatso zawo za Uzimu ndikukhala mamembala ochita chita ku Thupi la Kristu.

#### **7. KUSANKHA ATSOGOLERI: Macitidwe 14:23**

Pamene okhulupirira amakulu muuzimu, atsogoleri amudera amasankhidwa ndi Mulungu. Mpingo uli onse unakudza bungwe la baibulo limene linali la mawu, yochitachita, ndi yowona mene madera awo aalili. Ulamuliro okagwiritsa ntchito mphatso za Uzimu unaperekedwa ku mpingo, atsogoleri anasankhidwa m'mkati mwa mpingo. Pamene Paulo amasakha akulu akulu, anasankhidwa kuchokera mugulu la anthu, osati kutengedwa ku magawo ena.

**Cifukwa ca ici ndinakusiya iwe m'Krete, kuti ukalongosole zosowa, nukaike akuru m'midzi yonse, monga ndinakulamulira. (Tito 1:5)**

#### **8. MPINGO KUTSIMIKIDZIKA: Macitidwe 14:23; 16:40**

Pamene atsogoleri anali pamalopo ndikugwira bwino ntchito yawo, podalira zinthu zimene anthu amapereka ku mpingo. Njira yakale inaperekedwa kuchokera kwa wobzala mpingo kupita kwa atsogoleri atsopano amadera. Mpingo unatsimikidzika kapena kutsithidwa kupita kwa Ambuye pamene umagwira ntchito, thupi la okhulupirira amudera. Ngakhale mipingo yatsopano imafanana ndi mpingo wawukulu kumambali kwachiyanjano ndi utsogoleri, tsamadalira kuchokera kumpingo wawukulu. Anali mipingo yozinthandidza yokha pomwe amakwaniritsa kuchita ntchito ya Uthenga Wabwino posadalira zachuma zakumpingo wawukulu.

Mayendetsedwe azachuma amakodzeka ku mpingo watsopano potengera kuti anthuwo antha kuyendetsa zamalonda awo bwinobwino. Ngati mpingo ukulandira chithandidzo kuchokera ku mpingo wina, zipembedzo zina, kapena okhulupirira ochokera kumayiko ena ndiye kuti amakhala kuti akudalira mayiko amenewo. Ngati mpingo othandidza kapena zipembedzo

zina zikalephera kuthandiza, mpingo yatsopanoyi ndie kuti ilepheranso. Ngati ubale pakati pa mayiko suli bwino, mpingo udzakumana ndidzowawa pamene chithandizo kuchokera ku mpingo wina chachonsedwa.

Ambuye yemweo amene anatsitha madzi kukhala ku vinyo ndi kuchulutsa mkate ndi nsomba kudyetsa nkhamu la anthu ali ndikuthekera kukapedza ndalama moyenera kuti Uthenga Wabwino ukafikire aliyense. Paulo anakhanzikitsa mipingo yatsopano pa Mawu a Mulungu ndi pa Nthathwe, Yesu Kristu. Tsanawapedze iwowo muma bungwe kapena muzipembedzo dzina kapena mwayiye yenkha. Kukhala odalira simuphunzira kukhala odziyimira panokha.

## **9. UBALE KUPITIRIRA: Macitidwe 15:36; 18:23**

Ubale unapitirira pakati pa anthu obadwa mwatsopano, obzala mipingo (Paulo), ndi mayi mpingo (Yerusalemu). Ubale unakhadzikitsidwa pakati pa mipingo yatsopano ndi mipingo ina yodzungulira madera kuti apititse Uthenga Wabwino patsogolo.

## **10. KUPITIRIDZA UTHENGA:1 Atesalonika 1:8**

ku mpingo waku Atesalonika, “Mawu a Mulungu anafalikira konse” kuchokera kumipingo ya tsopano kufikira kwa anthu omwe sanafikiridwepo ndikupitiridza kulalikira zinachitika pakubzala mipingo yina yatsopano.

### **ZOLINGA ZA UTUMIKI**

Paulo anali ndi njira zake zolalikirira ndikubzala mpingo. Baibulo limanena za kukhunzidwa kwake ku Asia, Galatia, Macedonia, Acacia, ndi Spain, unli ufumu umodzi pa nthawi imeneyo. Phunzirani madera awa amene Paulo adabzala mipingo:

-Filipi: (Macitidwe a Atumwi 16) uwu unali dzinda wawukulu ku Makedoniya.

-Atesalonika: (Macitidwe a Atumwi 17:1-10) Uyu Unali dzina wawukulu komanso wochitira malonda.

-Korinto: (Macitidwe a Atumwi 18:1-11) unali dzina wadzamalonda ku Greece.

-Efeso: (Macitidwe a Atumwi 19:1-10) uku kunali kumene misewu ikulu ikulu ya Ufumu wa Aroma umachokera ku Roma kupita ku mawa. Efeso kunali doko ndi malo adzamalonda.

Zitsanzo izi zikukamba za zolinga 7 za utumiki:

### **MIDZINDA:**

Madera amene Paulo amakhanzikitsa mipingo kumene kunali likulu la Aroma, kutukuka kwa Aheleni, Malo akuluakulu a Ayuda, midzinda ikulu ikulu yazamalonda. Paulo anaziwa kuti antha kufikira anthu ochuluka mumadera omwe munali anthu madzana madzana.

Anadzindikilatso kuti kusitha kumayambira midzinda ikulu ikulu kenako kumapita kuma midzi. Malo ochitira malonda ndi malo okopa alendo makhala ndi anthu ambiri ochokera mayiko otsiyana tsiyana amene amabwera kudzachita malonda komanso kudzaona dzithu. Midzinda inali mitsewu yomwe mayendedwe awanthu amachitika. Pamene alendo amenewa amafikiridwa ndi Uthenga Wabwino, amatenga uthengawu pobwerera makwawo.

### **NTHAKA YOPANDA CHONDE**



Mu Mateyu 10, Yesu anawaudza ophunzira ake kuti asapite kwa a Samariya ndi akunja koma kwa ana a Israyeli. Nthawi inali yoyenera kwa ana a Israyeli. Magulu ena adzakhalabe anthaka mutsogolo. Pakati pa ayuda, ophunzira amayenera kukatumikira kwa anthu otayika. Amayenera kuyakhala kumeneko ndikugawana zimene amalandira ndi kusutha akakumna ndi anthu ulungama. Amayenera kukakhazikitsa mphamvu awo pama dera amene kunali anthu otayik ambiri.

Paulo nayeso anagwiritsa njira imeneyi. Pamene ayuda anakana Uthenga Wabwino, Paulo amachoka kwa ayuda kupita kwa akunja (Macitidwe 13:42-51). Pamene Atene anali atsakodzeke, Paulo anapita ku Korinto. Ku Korinto, Paulo anawasiya Ayuda kupita kwa anthu akunja. Ayuda otayika anakodwera ndipo ambiri anakhulupirira ndipo anabatidzidwa (Macitidwe 18:5-11). Mulungu anavomeredza ntchito za Paulo kudzera mu bvumbulutso kumuudza kuti akakhalabe mu Korinto ndikuti asaope kulalikira Kristu (Macitidwe 18:5-11). Pamene makachisi amidzi anamukana iye, Paulo nayamba kukhala pamodzi ndi amene anali otayika. Pamene masutso anatulutsa, iye anapita mdzinda wina.

### **ANTHU AKE OMWE:**

Paulo anali ndikhudzika pofikira anthu ake ndi Uthenga Wabwino:

**Abale, kufunitsa kwa mtima wanga ndi pemphero langa limene ndiwapempherera kwa Mulungu, ndilo, kuti apulumuke. (Aroma 10:1)**

### **ANTHU OSAFIKIRIDWA:**

Paulo anawonetsetsa kuti akafikire madera amene Yesu Kristu anali asanafikireko:

**Ndipo coteru ndinaciyesa cinthu caulemu kulalikira Uthenga Wabwino, pa malopo Kristu asanachulidwe kale, kuti ndisamange nyumba pa maziko amunthu wina;**

**Koma monga kwalembedwa, Iwo amene uthenga wace sunawafikire adzaona, ndipo iwo amene sanamve, adadziwitsa. (Aroma 15:20-21)**

Madera amene kulibeko mboni za Uthenga Wabwino akakhale oyamba kufikirako. Lembani fanizo la nkhosha mu Luka 10:13-14. Oyamaba kufikira anali nkhosha yosochera, osati zamunkhola.

### **ANTHU AMAGULU:**

Paulo anagwira ntchito ndi magulu a anthu otsiyana tsiyana ozungulira midzinda kapena zigawo zina. Mwachitsanzo, anatumikira kwa magulu onse a anthu achi Aheleni ndi Ayuda ku Antiokeya (Macitidwe 13:12). Pamene mwaphunzira mu mutu 6, gulu la anthu ndi ntundu, kapena gulu lililonse la chikhalidwe, kapena mbiri ya chikhalidwe. Ndichofunikira kukawona kaye mdzinda kapena chigawo kuti mudziwe magulu amenewa ndi kubzala mpingo moyenera.

Mwachitsanzo, mudera limodzi mudzinda wa United States muli anthu ambiri amene amayakhula chi Spanish, Oyakhula chizungu, ndi Mandarin Chinese. Kubweretsa kukudza, kudzabzala mipingo mumidzinda imeneyi mukuenera kudzafikira mtundu wa gulu la anthu awa, kudzabzala mpingo oyakhula Chichewa mudzina uwu sikungakhale kopindula chifukwa palibe amene amayakhula Chichewa mudzindawu. Ndichifukwa chake pobzala mpingo

mukuyenera kuyika chidwi pa anthu amimtundu iyi odzungulira madera awa, komanso osati mu dzinda mokha.

Kubzala mipingo modzungulira gulu la anthu kumakulitsa Uthenga Wabwino mwachangu. Mamembala a gulu la anthuonse amayakhula chilankhulo chimodzi ndi chikhalidwe chimodzi. Palibe chikhalidwe chomwe chingaphinje kufalitsidwa kwa Uthenga Wabwino. Padzifukwa izi, Uthenga Wabwino utha kufalitsidwa mwachangu.

Harvestime International Institute limakupasani phunziro lochedwa “Kuyang’ana zachilengedwe” chimene chimakuthandidzirani pakuona madera amene mungafikire ndi utumiki. Tikuganidza kuti mukapedze bukhuli kuti ikuthandidzireni pakubzala mpingo. Phunziro likuthandidzirani umu:

1. Kudziwa anthu amene mungawafikire. Ndi gulu la anthu liti lomwe limakhala mu dzinda kapena chigawo chimenecho? Mukufuna kufikira ndani? Chipembedzo chawo ndichiti, chikhalidwe ntundu kopanso mbiri yawo njotani?
2. Kudziwa zotsowa zawo za uzimu. Mwachitsanzo, kodi mpingo ukufunikira kwa anthu oyakhula Spanish mudzindawu? Mwina zosowa zatumikiridwa koma nanga oyakhula chi French mudzindawu sakutayidwa.
3. Dziwani otayika ofuna Uthenga Wabwino.
4. Dziwani njira ybwino yomwe mungagwiritse ntchito pofikira anthuwa. Kodi anangafikiridwe bwino motani? Ndani akuenera kuwafikira anthuwa?

#### **KUPEREKA UTHENGA WABWINO KU NKHAMU LA ANTHU:**

Paulo amapereka Uthenga wabwino ku nkhamu la anthu. Amatenga mwayi kulakhul ku nkhamu la anthu:

**Ndipo kunali pa Ikoniyo kuti analowa pamodzi m’sunagoge wa Ayuda, nalankhula kotere, kuti khamu lalikuru la Ayuda ndi Ahelene anakhulupirira. (Macitidwe a Atumwi 14:1)**

#### **KUPHUNZITSA MODZI MODZI:**

Paulo analalikira ku nkhamu la anthu komanso anaziwa kufuna kwakuyikidza moyo wake mwa amuna ochepe amene anakwanitse kuphunzitsa ena. Timoteo anali modzi mwa amuna ngatiso mene analiri Tito ndi Yohane Marko, amene anakanikidzidwapo kamodzi kukhala ophunzira (Macitidwe 15:36-60). Anali Paulo kudzera mwa Mzimu Woyera omwe unabvumbulutsa dongosolo la Mulungu kwa okhulupirira aliyense kuti akachuluke m’Mzimu (2 Timoteo 2:2).

Kugwira ntchito ndi okhulupirira ena ngati Barnaba ndi Sila, ngakhaleso ophunzira omwe anawaphunzitsa, kunachulukitsa kwambiri utumiki wa Tumwi Paulo. Paulendo wake wachiwiri ndi wachitatu wawutumiki, Paulo analemba thandidzo la ogwira naye ntchito amene anali dzika za madera amenewo pamene anapanda dongosolo kuti akagwire ntchito. Iyi ndi lamulo lofunikira kwambiri. Ma Africans atha kufikira ma Africans azawo bwino kwambiri. Indians atha kufikira antha awo bwinoso kwambiri. Asians atha kulowa mu continent yawo ndi Uthenga Wabwino. Amayakhula chirenkulocho, amavetsetsa chikhalidwe chawo ndi odziwaso kale mene moyo wawo watsiku ndi tsiku mene umayendera.

MAFUNSO OZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yapa mtima.

---

---

---

2. Njira 10 zozungulira zozabzala mpingo ndichani?

---

---

---

---

---

---

3. Kodi zolinga 7 za utumiki wa Tumwi Paulo zinali chani?

---

---

---

---

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

## MAPHUNZIRO OWONJEDZERA

1. Kulalikira ndi kubzala mpingo komwe kumachitika ndi Tumwi Paulo kumakambika kwambiri mumagawo atatu awulendo wa utumiki:

Ulendo oyamba: Macitidwe 13:1-14:28

Ulendo wachiwiri: Macitidwe 15:36-18:22

Ulendo wachitatu: Macitidwe 18:23-21:14

2. Phunzirani zambiri kubzala mpingo munjira zobweredza bweredza yomwe yagwiritsidwa ntchito mu dzinda uliwonse pakuonetsera zochitika zomwe zinachitika mu dzinda wa Efeso:

- Anthu kufikiridwa: Macitidwe 18:19; 19:1,8,9
- Uthenga Wabwino Kuperekedwa: Macitidwe 19:4,9,10
- Overa atembenuka Mtima: Macitidwe 19:5,18
- Okhulupirira kubwera Pamodzi: Macitidwe 19:9-10
- Chikhulupiriro Kutsikidzika: Macitidwe 20:20,27
- Kusankha Atsogoleri: Macitidwe 20:17,28; 1 Timoteo 1:3,4
- Mpingo kutsimikidzika: Macitidwe 20:17; Aefeso 1:1-3,15,16

Izi ndi njira zomwe mungasatire pobzala mpingo:

### KUKODZEKERA MU UZIMU:

- \_\_\_ Ndakhala nthawi yayitali ndikulingalira ndiku pemphera zokhunzana ndikubzala mpingo.
- \_\_\_ Ndili ndikutsimikidzika mtima kuti Mulungu akunditsogolera kukabzala mpingowu.
- \_\_\_ Sindikuchita izi kuti ndikakondweretse anthu.
- \_\_\_ Ndili masophenya achifukwa chomwe mpingo ukufunikira ndipo ukakhala odabwitsa.

(Lembani izi mu “Fundo ya Cholinga” mpingo uliwonse uli cholinga chake komanso chodabwitsa kuti ukakwaniritse mkatimkati mwa zolinga za Mulungu kuti dziko lonse lapansi likafikiridwe ndi Uthenga Wabwino. Phunziro lamu The Harvestime International Institute “Kuchita ndi Zolinga” likakuphunzitsani kudziwa cholinga chanu ndi kuti mukachinene ndi mawu oveka bwino.)

- \_\_\_ Ndikukhulupirira kuti ndili nazo zondiyeneredza za uzimu kukhala obzala mpingo.

Awa ndizinthu zomuyeneredza munthu zomwe zili zofunikira kwa munthu yemwe akufuna kukhala obzala mpingo. Akuyenera kukhala:

- Oyitanidwa ndi Mulungu to ntchito yoyikidzika ya Utumiki.
- Odzadza ndi mphatso za Uzimu ngati tsogoleri kuti akadzadze ena kuntchito ya utumiki
- Akakhala ndizomuyeneredza za baibulo ku ntchito ya tsogoleri mu 1 Timoteo 3:17.
- Akhale odzipansa ulemu.
- Akhale opirira pamene anthu amusiya ndi kudzokhumudwitsa kuti adzakhumudwe.
- Odziwa kusatira nyengo ndi zikhalidwe zotsiyana.

- Ofuna ndi kuthekera kotsogolera anthu.
- Munthu wachikhulupiriro, okhulupirira Mulungu kuti achita dzithu zazikulu.
- Odzipereka kuntchito ya kubzala mpingo.

(Ngati ali okwatira)

\_\_ Banja lonse likhale muumodzi ndi masophenyawa.

**KUTSAKHA MALO OFUNIKAWO:**

\_\_ Ndapepherera za malo omwe ndikadzale mpingo.

\_\_ Ndawunikira bwino bwino zamomwe kuliri.

(Gwiritsani ntchito Harvestime International Institute phunziro lochedwa “Kuwunikira za Malo” kucholinga chanucho. Zimafotokodza za momwe mungagwiritsire fundo zotsiyansiyana podziwa malowo ndikuti likuthandizirani momwe madera akodzekerera kulalikiridwa komanso kubzala mpingo. Zikufotokodza za momwe mungawadziwire gulu la anthu, momwe liriri deralo, dziko, kapena chigawo cha dziko lonse pakukodzekerera kuti mukalowemo ndi Uthenga Wabwino.)

\_\_ Mene malo ampingo akambidwe kale.

(Pezani map kuti akuthandidzeni pochita izi, pamodzi ndi fundo zomwe mwapedza mu kuwunikira za malowo.)

\_\_ Ndamallidza kupanga kafukufuku wa mdera kwa anthu okwana 100 omwe alibe mpingo muderali.

(Kafukufuku uyu akuthandizirani kuchita ulalikira wa modzi modzi ndikuziwa zotsowa za Uzimu za anthu ndi madera a anthu otayika.)

Iyi ndi form yomwe mungafunikire pochita kafukufuku wanu.

**KAFUKUFUKU WAMUDERA**

Tsiku lomwe munapita: \_\_\_\_\_

Dzina: \_\_\_\_\_

Komwe amakhala: \_\_\_\_\_

Mamembala okhala nyumba: Abambo: \_\_\_\_\_ Amayi: \_\_\_\_\_ Nambala ya ana \_\_\_\_\_.

1. Kodi ndinu membala wochitachita ku church? (Funso ili litha kuthera ku kulalikira. Nsimukufuna kuwachosa anthu kumipingo komwe amapita.)  
 \_\_\_\_ ndi membala ochitachita. \_\_\_\_ ndi membala osachitachita.
2. Kodi mumaganidza kuti chotsowa chachikulu cha anthu muderali ndi chani? (Mayankho omwe mungalandire pa funso iyi zikuthandizirani kudziwa utumiki omwe ukufunikira

kumalo amenewa. Zimakuthandizirani kudziwa mphamvu zomwe zikufunika pakulalikira kudzotsowa za anthu.)

---

3. Mukuganidza kuti ndichifukwa chani anthu ambiri ku dera lino tsapita ku mpingo?  
(Funso likupereka kuthekera kothana ndizowirungula zomwe anthu ali nazo.)

---

4. Ngati busa wa mpingo watsopano mudera lanu, ndichinthu chiti chomwe mungafuna takuchitirani inu ndi apa banja lanu? (Funso limakupasani inu mwayi oti mukayambe kutumikira banjali, ndipakutha pa cholinga chaku lalikira.)

---

5. Kodi muli ndi adzanu kapena achibale omwe angakondwe ndi mpingo ngati wathuwu.  
(Ichi chikapasani kuwonjedzera kufikila anthu ena powalalikira.)

---

**Onani zina za omwe mukuwafunsawo:** \_\_\_\_\_ ali  
ndimalingaliro abwino. \_\_\_\_\_ amachawi kupingo  
wina. \_\_\_\_\_ akufuna mutabweranso. \_\_\_\_\_  
akufuna baibulo. \_\_\_\_\_ akufuna maphunziro ena  
apadera a baibulo \_\_\_\_\_

### **KUTSOKHANITSA ZIPHONA ZA PA MPINGO**

Lembani mayina a anthu omwe angalowe nawo mugulu la mapemphero kupingo watsopano:

---

---

Dziwana anthu amene angakhale ziphona zapa mpingo watsopano kupephero. Akuyenera kukhala okhulupirira omwe atembenuka mtima kumene mu dera limenelo kapena okhulupirira okwima amene mungawatumidze ku likuli la mpingo wanu kuti akathe kuthandidzira kubzala mpingo wina madera ena osakhidwa.

---

---

\_\_\_ Tasankha dzina la mpingo.

\_\_\_ Tiri ndi mfundo ya cholinga.

\_\_\_ Talemba fundo zophunzitsira zomwe zikukamba za zomwe mpingo umakhulupirira.

\_\_\_ Tamalidza mapepala ofunikira ku boma pobzala mpingo wanthu watsopano.

\_\_\_ Takwaniritsa zofunikira zachipembedzo

\_\_\_ Talemba zofunikira zoti munthu akhale membala wathu.

\_\_\_ Takhakitsa thumba laza chuma.

(Muphunziro la The Harvestime International Institute “*kuchita ndi zolinga*” imanena momwe mungachitire izi.)

### **KUKHADZIKITSA ATSOGOLERI A MPINGO:**

\_\_\_ Taona atsogoleri omwe akufunika mwachangu kuti tikayambe mpingo.

\_\_\_ Taona utsogoleri omwe udzafunike kutsogolo ku mpingo.

\_\_\_ Tikubweretsa pamodzi ziphona kuti zikagwire ku utumiki malingana ndi mphatso zawo za uzimu.

(Phunziro la The Harvestime International Institute “*njira yakubweretsa pamodzi*” idzakuthandizani kuchita izi).

Phunziro la The Harvestime International Institute “*kuchita ndi zolinga*” limapereka momwe maudindo a utumiki akuyenera kukhalira monga umu:

- Abusa
- Wachiwiri kwa abusa
- Atumwi
- Aneneri
- Aphunzitsi
- Akulu ampingo
- Madikoni
- Wapapando woyangaira ma pephero
- Otsogolera maphunziro achikristu
- Otsogolera utumiki ndi cholinga chake
- Otsogolera utumiki wa amuna
- Otsogolera utumiki wa akadzi
- Otsogolera nyimo
- Mlembi wa mpingo
- Otsogolera za chuma
- Otsogolera pomwe pawonongeka mpingo
- Otsogolera zida zamagetsi
- Ma asha
- Wapapando ofalitsa mauthenga
- Ma udindo ena apadera

Phunziro la The Harvestime International Institute “*Malamulo ogwirira ntchito amubaibulo*” ikakutsogolererani inu pakusakha komanso kutukula atsogoleri a mpingo. Imapereka

malamulo amumalemba a baibulo mene munthu angakhalire tsogoleri wabwino ndi wotsatira wabwino.

### **KUSANKHA MALO OKUMANIRANA:**

\_\_Malo omwe tasayakha kuti tikumane ndiodziwika ndi aliyese wamuderali (anthu antha kuwaona ndipo anthaso kuwapedzatso motsavuta).

\_\_Ndiwosavuta kufikirako (anthu atha kufikirako motsavuta pogwiritsa ntchito magalimoto amalonda kapena kuyenda basi).

\_\_Malowo pali malo otsungira magalimoto (ngati mamembala angabwere pa galimoto ku mpingo).

\_\_Malowo ali manja mwa maboma ang'ono ang'ono.

\_\_Mangalande ndiwokwanira (kupewa kutsefukira).

\_\_Palibe mitsokho yotsalipiridwa, ngongole, kuti mudzalipira inuyo.

\_\_Malowo akadali abwino.

(Lingalirani zinthu zomwe zingayenere kuchitika pansu, kudenga, khoma, madzenera, zitseko, kuti malowo akagwire ntchito. Ngatiso mutalingalira pogula malowo, mupedza odzomanga manga adzawawunikire malowo.)

\_\_Kodi malowo ndiwokwanira pa nthawi ino ndikuti mungazathe kukulitsa kutsogoloku? Izi ndi dzina zofunikira kuwunikira popedza maloanu:

- Chipinda chachikulu chomwe chingagwire ntchito polambira, kupephera, ndikukumana.
- Damu la ubatidzo
- Chipinda chowerengera cha abusa
- Chipinda cha mlembi
- Malo ochedzera ana
- Malo ophunzitsira ana kapena malo oohunzirira baibulo.
- Kophikira
- Malo ogonapo.

\_\_Kodi malowo mungathe kuwasitha kukhala apa mwamba? Onani ngati zinalembedwa mabukhu.

Izi ndi dzina mwa ubwino ndi kuyipa kwa malo ambiri amene amagwiritsidwa ntchito ndi mpingo:

### **NYUMBA YA MPINGO:**

Ubwino:

- Mumapanga mibindikiro.
- Tsimulipira ndalama.
- Njira yamu Chipangano Chatsopano.
- Pamene anthu ambiri akubwera, zimalimbikitsa kuti magulu aziphona mumapephero akafune malo akulu kuti muzikulabe.



Kuyipa:

- Ena samava bwino kubwera kunyumba pokhapokha atamudziwa mwini wake wa nyumbayo.
- Kulibe malo ambiri otsungira galimoto ndi okhalapo anthu.
- Zimakhala zowawa kwa eni nyumba kuti aziyipereka sabata liri lonse.
- Kudziwika (malo apa nyumba) nthawi kutha kukhala kovuta. Zintha kukhala zovuta kukupedza kumaloko.

### **KUPEDZA HOLO LALIKIKULU DERALO:**

Malo amenewa antha kukhala malo akulu okumanirana mudzinawo, amene anthu ambiri amachitirako zochitika chitika, malo a club, pasukulu, malo ogonako alendo. (ziwani kuti: pakusankha hollo mudera, pokwiritsa ntchito malo ochititsira maliro tsioyenera. Anthu amene amagwiritsa ntchito malo ochititsira maliro zintha kumawabweretsera zikumbutso za anthu omwe anamwalira.)

Ubwino:

- Kumakhala malo ambiri okhala komanso bwalo lalikuli lotsungira magalimoto.
- Kudziwa malowo tsikuvuta
- Anthu ambiri amadziwa kuti hollo ili mbali yakuti.
- Kuli chipinda choti mungathe kukula mutsanapedze malo okhazikika.

Kuyipa:

- Ndikovuta kutsamalira malowa chifukwa malowa amagwiritsidwa ntchito ndi anthu ambiri.
- Zokongoletsera ndi zina zintha kukhala zotsagwirizana ndi mapephero.
- Kupedza mtsiku ochitira mapephero kutha kukhala kovuta chifukwa choti ena apedza kale.
- Padzifunikira mweni wake kapena wantchito wapamalopo kuti atsegule holloyo.

### **KUGAWANA MALO A MPINGO NDI ANTHU ENA:**

Ubwino:

- Pali malo okwanira okhalapo komanso otsungira galimoto
- Anthu ambiri amadziwapo.
- Malo okwanira kuti mukakule pamene musanagule malo anu
- Mpingo umapereka chithuzi thunzi chabwino polambira.

Kuyipa:

- Kovuta kusamalira malo a mpingo chifukwa pa mpingopo pakugwiritsidwa ntchito ndi anthu ambiri.
- Kupanga dongosolo kovuta chifukwa choti anthu ena amakhala kuti apetenga kale patsikulo.

### **KUGULA NYUMBA KUYITSINTHA KUKHALA MPINGO NDI KUYIBWEDZERA KUKHALA YA MUNTHU:**

Ubwino:

- Munthawi zambiri, kotsavuta kutenga ngongole ya nyumba kuposa ya mpingo. Kenako muntha kuyitsitha kuti ikakhale nyuma ya abusa pambuyo pake. Pali zophinya zochulukira poyika ndalama kuchithu.
- Pena, anthu odzungulira amabvomeredza akadziwa kuti mpingo ukungogwiritsa ntchito kwaka nthawi kochepa.
- Mumapanga kuti ankhale malo ombedzera.

Kuyipa:

- Mpingo umakhala ndi chidzolowedzi chomakhadzikitsa malo a mpingo.
- Pamakhala kuphinya pakukula.
- Kuchepa kwamalo.

### **KUPANGA DONGOSOLO NDI KUCHITA MAPEPHERO KOYAMBA:**

\_\_Tayika tsiku, nthawi, ndi dera lochitira mapephero koyamba.

\_\_Talengedzetsa muderali mokwanira.

(Pakulengedza muyikemo Mawu apakamwa, makanema, nyumba zowulusira mawu, mapepala ang'ono ang'ono, maposita, newspaper, lamnya, zizindikiro ndizina zambiri, potengera mene derali liriri komanso zachuma zano.

\_\_Takhazikitsa mapephero oyamba kukafikira omwe Sali okhulupirira ndi kuwapatsa mwayi waku lambira, kulalikira ndi kuchitapo kathu.

### **KUCHITA MAPEPHERO MOWIRIKIDZA:**

Zoyenera kuchita pamapephero:

- Kulambira: izi zikuyenera kukhala chokhazikika, kukala mawu, kutsogozedwa ndi Mzimu Woyera, ndi dzina zoyenera. Poyimba nyimbo mukuyenera kuwaphatikizamo anthu amene abwera gulu la athu ngati akwaya, oyimba, ndizina zambiri.
- Chopereka.
- Gonero
- Kuwerenga, kulalikira ndi kuphunzitsa mawu a Mulungu. Izi zikuenera kusatira ndondomeko yomwe ilipo ya kulalikira ndi kutsogolera ndie mowirikidza muzikazutsa anthu otembenuka mtima atsopano ndikuwakodzekeretsa ku ntchito ya utumiki.
- Ubatizo wa madzi.
- Mwayi odzipereka ndi kukhala kwa Ambuye kwa onse okhulupirira ndi otsakhulupirira.
- Kugwira ntchito kwa Mphatso za Mzimu Woyera.
- Utumiki wa thupi, pamene mamembala akuyenera kutumikirana wina ndi mzake.
- Kugwiritsa ntchito njira zamakono popereka Uthenga Wabwino ngati zowonera ndi zovera, mafilimu, kupanga zolembe, ziwonetsero.

**Awa ndi maganidzo omwe mungapangire dongosolo la mapephero kuti mukafikire anthu otsapulumuka:**

-Khazikikani padzotsowa dzawo: Polengedzetsa “Mapephero odzadza ndi Mzimu” izi tsizikabweretsa anthu otsapululumuka ndipotso dzikathawitsa anthu ambiri. Koma khazikikani, padzotsowa zawo. Mwachitsanzo, muntha kulengedzetsa mapephero anu pamutu oti “Mene mungagonjetsere nyengo zovuta pa Moyo wanu.”

-Khalani zinthu zonse kwa onse kuti mukapedze zina: Onani 1 Akorinto 10:19-23. Palibe mulingo omwe -mungafikirire anthu otsapululumuka. Malo mopephera “Kodi ndikalalikire zokhudza chani?” Pepherani, “Kodi ndikalikira ndani?” onani anthu amene Mulungu akuwabweretsa kuchitsamaliro mwanu.

-Uthenga wanu ukhale woti “Khani Ya Bwino” Ya Uthenga Wabwino: Tsi Uthenga Wabwino pokhapokha itakhala khani ya bwino. Wunikirani mafunso otsatirawa:

- Kodi mutu wa uthengawu zikutanthauza kuti ndili ndi khani yabwino kukagawana nawo?
- Kodi uthengawu ukupereka thandizo logwirika kuchokera ku Mawu a Mulungu?
- Kodi njira yosavuta yoperekeru Uthengawu ndi Yiti? (yosavuta sikuti kusaladza. Yesu anapereka uthenga mosavuta koma uthenga wamphamvu).
- Kodi ndingapereke bwanji kuti ukachite kwakukulu? (Afalitsi anava kuchokera kwa ena ndipo sizinapindulire. Ophunzira anaphunzitsa monga mene anaphunzirira, ndipo miyoyo yawo inasitha. Mugawane mwa modzi modzi, mwachulungamo ndi kusindika ndiku khunzika.)
- Kodi njira yosangala yonenera ndi iti? (Yesu anagwiritsa ntchito nkhani zotsangalatsa za anthu ndima fanizo ovetsetseka ndi munthu wamba.)

-Chepetsani zolengedza za mpingo: izi zinthu kulembedwa mapepala kapena njira yina.

Anthu otsapululumuka amabwera chifukwa choti ali ndi zotsawa mu miyoyo yawo, otsati kudzavera zolengedza, zoti muchita.

-Tsankhani gawo lamalemba ndi nyimo mosamala: muwonetsetse kuti zikukhuza kwambiri anthu otsapululumuka ndipo zomwe zili zotsavuta kuvetsetsa. Mwachitsadzo, malemba oti “Kumenyetsa ana ang’ono kukhoma” mawu neneri a Chipangano Chakale tsakakhala opweka kuti munthu otsakhulupirira akawavesese. Onetsetsani kuti nyimbo ndizotsavuta kuvetsetsa kwa anthu otsapululumuka.

-Perekani mwayi kuti ayakhe: nthawi ili yonse perekani mwayi kuti alandire Yesu Kristu ndikuembedza kuti anthu ayankha.

### **KUKHANZIKITSA MADONGOTSOLO OPITIRIRA KUNTCHITO YA UTUMIKI:**

Mukuenera kupitiridza kuyika, kuchita, ndi kuwunikira zolinga zakutsogolo zotukula mpingo. Cholinga cheni cheni cha dongosolo ili, zoona, zikuenera kukhala zoti kulalikira kukuyenera kupita pa tsogolo, kuphunzitsa, ndiku bzala mipingo. Mutu 14 wa phunziro ili ndi The Harvestime International Institute “Kuchita ndizolinga” ikuthandizirani inu pakukhazikika, kuchita ndikuwunikira ma dongosolo anu.

Ngati kuli kale mipingo yina muderali kumene mukufuna kukabzala mpingo watsopani, musakhale opikitsana. Kalata kapena kuendera azibusa amipingo yinayo kukakupasani inu kulimbika mtima uku:

*“chonde ndiloleri ndizifotokedze ndekha. Ine*

*ndine\_\_\_\_\_ (dzina)\_\_\_\_\_*

*mukuyimirira\_\_\_\_\_ (dzina la mpingo wanu) \_\_\_\_\_.*

*Anthu oyimirira mpingo wanthu abzalakhulana ndi anthu amudera lino ndicholinga chakugawana nawo mawu a Mulungu, ndikuwina otembenuka atsopano, ndikuwakhankitsa mumipingo yamidzi.*

*(Fotokodzani kwambiri za cholinga chanu pa fundo iyi: kodi mpingo watsopanowu ukatumikira kwa magulu a anthu oyikidzika kapena midzi? Kodi cholinga chodabwitsa cheni cheni mudzimu ndichani?)*

*Pamene mukuyankhulana ndi anthu amudizimu, ndizotheka kuti mamembala ampingo wanu adzafikiridwa. Tsicholinga chathu kuti tikakhuze mamembala ampingo yina kuti akasiye mipingo yanu. Chokhumba chathu ndikugawa Uthenga Wabwino ndi anthu amene sanafikiridwepo mudzi mwanu ndi kugwira ntchito limodzi ndi mpingo wanu pakufikira dera limeneli mwa Ambuye wathu Yesu Kristu.”*

## CHAPUTALA 22

### KUBZALA MPINGO: KUCHULUKITSA

#### ZOLINGA:

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba vesi yotsogorera.
- Kufotokodza “kukula mkati mwa mpingo.”
- Kufotokodza “kuchulukitsa kwa mpingo.”
- Kufotokodza “kuwonjedzera kukula kwa mpingo.”
- Kufotokodza “kuwoloka kukudza mpingo.”

#### VESI YAPA YOTSOGOLERA:

**Kucokera kwa Iye amene thupi lonse, lothandidzidwa pamodzi mwa mfundo ndi mitsepha, likula ndi makulidwe a Mulungu. (Akolose 2:19)**

#### CHIYAMBI

Pakuntha pabzala mpingo watsopano, ukuenera kukayenda mukukula kudzera mundondomeko yakuchulukitsa yamu Chipangano Chatsopano. Izi ndizofunika kwambiri ngati mpingo ungakhale waphamvu pakulalikira mudera lake komanso ku dziko lapansi. Chaputala ichi ikufotokodza mitundu yakukula yomwe mpingo ukuenera kuyendamo: mkati, kuwonjedzera, kukulutsa ndi kubweretsa kukula mu mpingo.

#### KUKULA MKATI MWA MPINGO

Pamene tikukamba zakukula mkati mwa mpingo, tikutathauza kukula muuzimu ndi kukula kwa mamembala ake. Mpingo umakula muuzimu molingana ndi mmene mma membala ake akukulira.

Paulo amanena kunjira iyi, mofanidzira kukula mkati mwa thupi:

**Kucokera kwa Iye amene thupi lonse, lothandidzidwa pamodzi mwa mfundo ndi mitsepha, likula ndi makulidwe a Mulungu. (Akolose 2:19)**

“Kuonjedzera kwa Mulungu kutanthauna kuti kukula ku uzimu. Pamene mamembala akukula muuzimu, mpingo umayenda mukukula mkati mwa mamembala. Thupi lonse limatsangalala ndi kukula ndi makulidwe a Mulungu. Kukula muzimu ndikukula maganiziridwe a awuzimu chimene chimapangitsa kukula moyo wa Kristu mwa okhulupirira. Ndikukula muchidziwitso cha Kristu:

**Koma kulani m’cisomo ndi cizindikiritso ca Ambuye wathu Mpulumutsi Yesu Kristu. (2 Petro 3:18)**

Ndikukula mwa Yesu:

**Koma ndi kucita zoonza mwa cikondi tikakule m'zinthu zonse, kufikira Iye amene ali mutu ndiye Kristu. (Aefeso 5:15)**

Kukula mzimu ndiye kuti kuchope kuzilakolako za thupi ndi kukuza moyo wa Kristu mwa inu:

**Iyeyo ayenera kukula, koma ine ndicepe (Yohane 3:30)**

Kukula muuzimu sikumangobwera kokha ngati mene munthu wakhallira nthawi yayitali ngati okhulupirira. Ndizotsatira zakukula kwa moyo wa Kristu mwa okhulupirira.

Umboni wakukula muuzimu ndi:

1. Kukula muchidziwitso cha uzimu.
2. Kagwiritsidwe ntchito koyenera kwachidziwitso ku moyo ndi ku utumiki.
3. Kukhala munthu otsangalala ndi zinthu za uzimu
4. Chikondi chachikulu pa Mulungu ndi anthu ena
5. Kukula mudzoyeneredza za Moyo wa Kristu.
6. Makulidwe azokhumba ndi kuthekera kogawana Uthenga Wabwino ndi ena.
7. Kukudza ndikugwiritsa ntchito mphatso za uzimu pafupi pafupi.

Kukula ndichilengedwe cha moyo wathupi. Ngati pali moyo wauzimu pa mpingo, kukula mkati mkati kudzachitika ngakhalenso kuchulukitsa, kuwonjedzera ndi kubwera kukula mpingo.

## **KUKULA KOCHULUKITSA**

Kukula kochulukitsa kumachitika pamene okhulupirira atembenudza mtima munthu kupita kwa Kristu ndikuwabweretsa kuchiyanjano ndi anthu mupingo mwawo momo. Ichi chimabweretsa kukula mu nambala yampingo muderalo. Kukula kochulukitsa kukuenera kukhala ndicholinga chongokulitsa Ufumu wa Mulungu. Ngati wachiwiri wawonjedzera mamembala 100 atsopano kuchokera mpingo woyamba ngati trasifa, kukula kwa Ufumu sikunachitike apa. Kwangochitika kukula kwama membala pa mpingo wachiwiri koma osati kuchulukitsa Ufumu wa Mulungu. Ufumu wa Mulungu umakula pokha pokha ngati wina walandira Yesu Kristu ndipo naphunzitsidwa kukhala membala wa Thupi la Kristu woyenera.

Kukula kwakuchulukitsa kwa mpingo kwafotokodzeredwa mu bukhu la Macitidwe a Atumwi:

**Ndipo m' masiku awa anaimirira Petro pakati pa abale, nati (gulu la anthu losonkhana pamalo pomwe ndilo ngati zana limodzi ndi makumi awiri). (Macitidwe a Atumwi 1:15)**

Mpingo unayamba pa chipinda chapamwamba ndi tundu wa anthu ophunzira 120. Patsiku lapatsaka 3,000 anawonjedzekerera kumpingo waku Yerusalemu.

**Pamenepo iwo amene analandira mau ace anabatizidwa; ndipo anawonjedzera tsiku lomwelo anthu ngati zikwi zitatu. (Macitidwe a Atumwi 2:41)**

Atatha pasaka, kukula kochulukitsa kumachitika tsiku ndi tsiku:

**Ndipo Ambuye anawaonjedzera tsiku ndi tsiku amene akuti apulumutsidwe.  
(Macitidwe a Atumwi 2:47)**

Nambala ya amuna mu mpingo waku Yerusalemu inakula kufika 5,000. Kuwerenga uku sikunaphatikize adzimayi ndi ana amene anali gawo la mpingo:

**Koma ambiri a iwo amene adamva mau anakhulupirira; ndipo ciwerengero ca amuna cinali ngati zikwi zisanu. (Macitidwe 4:4)**

Nthawi zambiri, anthu ambiri amawonjedzekera ku mpingo:

**Ndipo makamaka anaonjedzedwa kwa Ambuye okhulupirira ambiri, ndiwo amuna ndi akadzi. (Macitidwe 5:14)**

Mawu anaphatikidzidwa koyamba anagwiritsidwa nthito kufotokodza za kuchulukitsa kwa mpingo. Mwachangu kukula kunachitika kwambiri mawu amenewa “kuchulukitsa” anagwiritsidwa ntchito:

**Ndipo mau a Mulungu anakula; ndipo ciwerengero cha akuphunzira cidacurukatu ku Yerusalemu... (Macitidwe 6:7)**

Kuchokera pa fundo iyi, Macitidwe a Atumwa anakamba zakuchulukana kwa mpingo yamadera ndi mamembala ake amadera mipingo yaku Yerusalemu. Mipingo yatsopano inadzalidwa paliponse pakati pamadera odziwika kudziko lapansi kudzaka zotsakwana 40. Mwachitsanzo, ku Samariya...

**...koma pamene anakhulupirira Filipino wakulalikira Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu ndi dzina laYesu Kristu anabatizidwa, amuna ndi akazi. (Macitidwe 8:12)**

Mipingo ku Yudeya, Galireya, Samariya, Luda, Sarona ndi Yopa onse anakumana ndi kukula kochulukitsa:

**Pamenepo ndipo mpingo wa m'Yudeya lonse ndi Galileya ndi Samariya unali nao mtendere nukhazikika; ndipo unayenda m'kuopa kwa Ambuye ndi m'cithonhozo ca Mzimu Woyera, nucuruka. (Macitidwe 9:31)**

**Ndipo anamuona iye onse akukhala ku Luda ndi ku Sarona, natembenukira kwa Ambuye amenewa.**

**Ndipo kudadziwika ku Yopa konse: Ndipo ambiri anakhulupirira Ambuye. (Macitidwe 9:31)**

Kunali kukula mu mpingo waku Antiokeya (Macitidwe a Atumwi 11:21,24,26); Ikoniyo (Macitidwe a Atumwi 14:1); Derbe (Macitidwe a Atumwi 14:20-21); Galatiya (Macitidwe 16:5); Filipi (Macitidwe a Atumwi 16:14); Atesalonika (Macitidwe a Atumwi 17:4); Bereya (Macitidwe a Atumwi 17:12) ndi Ankolito (Macitidwe a Atumwi 18:8-11).

Mpingo unakula chifukwa:

-Maso phenya awuzimu Yohane 4:25

-Kutumikira madera mwa anthu otayika ndikusunga nthawi: Mateyu 10:5-6,14; Macitidwe a Atumwi 9:20-31; 16:6

-Njira ya “Kupita” kuposa “Kubwera”: Anapita kwa anthu malo modikira kuti anthuwo abwera ku mpingo.

-Okhulupirira onse amabala zipatso: Macitidwe a Atumwi 8:4

-Kugwiritsa ntchito njira zamalonda: Mamembala anawina achibale ndi azawo. Uthenga wabwino unafalikira unafalikira mwachangu pogwiritsa ntchito njira zamalonda momwe amaziwana ndi anthu.

-Kugwiritsa ntchito njira zomwe Yesu Kristu anagwiritsa: bukhu lonse la Macitidwe a Atumwi, mpingo oyamba unagwiritsa ntchito njira zomwe anaphunzitsa ndikuwonetsera Yesu Kristu. Analalikira Uthenga Wabwino, kuphunzitsa mau, kubatiza okhulupirira atsopano, ndikuphunzitsa ophunzira mwatsopano (Mateyu 28:19-20).

-Gulu la Chipangano Chatsopano: Magulu anali ofunikira kwambiri paku chulukitsa utumiki mu Chipangano Chatsopano. Paulo anaphunzitsa gulu la anthu apadera dera omwe anali ophunzira pakuwonjedzera ma sukulu (Macitidwe 19:9). Paulo anaphunzitsa masunagoga a Ayuda ndi achikunja (macitidwe 13:42). Magulu ang’ono ang’ono munyumba zawo (Macitidwe 12).

-Nyumba ili yonse imakhala pakati pochitira utumiki: Nyumba ili yonse inakhala pakati pochitira mapephero, kulalikira, kuphunzitsa, kuchilitsa ndi kumasula.

-Utumiki wa Mzimu Woyera: Mimu woyera ndi mphamvu yomwe imapereka chikumbumtima cha uchimo mwa amuna ndi azimai ndikuwakakamidza kuti alandire Uthenga Wabwino. Ichi chimabweretsa kutembenuka mtima kwa atsopano ndipo kumabweresa kuchuluka kwa mpingo.

-Mphatso za Uzimu: Kukula kwa munthu kumafunikira kukwima kwa mafupa komwe kumathandizira kuchulukana kwama cellozi. Kuti Thupi la Kristu likakule, ndondomeko ndiyofunika, Yesu anati, zotuta zaphya, koma ogwira ntchito ndiochepe, ngati ogwira ntchito ndiochepe, ndiye kuti akuenera kubwera pamodzi mwachindunji kuti akatute zokolola.

## **KUKULA KOKUDZA**

Kukula kokudza kumachitika pamene mpingo wayambitsa mpingo wina muchikhalidwe cha anthu omwewo. Mpingo watsopano umakhala okudza “mayi” mpingo, ngati mwana wakuthupi ndikukula kwa makolo ake. Mbiri yakukula mu bukhu la Macitidwe a Atumwi imawonesera pamene anayamba ku Yerusalemu mpingo waku Yudeya, Galireya, Luda, Saroni, ndi Yopa. Iyi inali mitundu yofanana mpingo wa Ayuda.

Pali njira 4 zomwe mpingo watsopano umayambira:



1. Mpingo umodzi umayambitsa mpingo wina.
2. Mipingo yambiri imagwiridzana kuti ayambitse mpingo wina.
3. Mpingo wawukulu kuwugawa kukhala mipingo iwiri kapena mipingo yambiri yosiyana.
4. Okhulupirira modzi kutumidzidwa kudera lina kuti akayambitse mpingo. Munthu modzi amene ali ndi mphatso ya Uzimu ya mtumwi ndi amene amagwiritsidwa ntchito pa nthawi iyi. Mtumwi Paulo ndichitsanzo. Munthu uyu nthawi zina amantchedwa “obzala mpingo”.

Mu chilichose cha ichi, kuchulukitsa kumachitika podzera kukudza Uthenga Wabwino poyambitsa Thupi lina latsopano la okhulupirira.

Mipingo yatsopano itha kukhala magawo atatu akukudza:

1. Mipingo kutumikira kutundu wa anthu amudera osakhika:

Mipingo iyi imakhazikisidwa kuti ikatumikire anthu osakhika amumadera, midzi, kapena midzinda. Kutha kukhala zotsatira zomwe utumiki omwe wadutsa gulu la anthu okhulupirira atsopano amuderalo. Atha kukhazikitsidwa kuti akatumikire malo omwe sanafikiridwe or dera la anthu otayika.

2. Mipingo kutumikira ku gulu la ntundu wa anthu otsakhika:

Ziyanjano izi zimatumikira ku gulu la ntundu wa anthu omwe ali achikhalidwe chimodzi, chikhulupiriro chimodzi ndi chirankhulo chimodzi. Mwachitsanzo, mpingo utha kuyambitsidwa kwa anthu amene amayakhula chi Spanish ndipo zamatha kuva chizungu chomwe chimayakhulidwa ndi “Mayi” mpingo. Zitsanzo zina zitha kukhala mpingo kwa anthu aku Asia womwe ali malo othawa nkhongo kapena anthu aku India amene akukhala kwa America madera awo.

3. Mpingo ndicholinga chapadera dera:

Mpingo utha kukhazikisidwa ndicholinga chapa dera dera. Mwachitsanzo, mpingo utha kudzalidwe pafupi ndi sukulu ya ukachenjedwe kuti ukatumikira ana ophunzira pa sukulupo basi.

## **KUKUDZA KOWOLOKA**

Kukudza kowoloka kumachitika pamene mpingo wawonjedzekereka kufika kudziko, malo okumaniramu anthu, tundu wa anthu, kuti mukadzale mpingo watsopano muchikhalidwe chotsiyana. Mawu oti “Kuwoloka” amagwiritsa ntchito pamene dongosolo la chitika “Mlatho” umakhazikitsidwa kuchokera ku chikhalidwe china kupita china kuti Uthenga wabwino ukaperekedwe.

Njira zamakono zamayendedwe ndi zofalitsira uthenga zakudza kwambiri kuthekera kwa mpingo kuti ukakule powolokera ngakhale madera ena ang'ono ang'ono. Kukuda kowoloka kunali mbali imodzi ya dongosolo la Ambuye Yesu pakukudza Uthenga Wabwino kupita ku dziko lonse lapansi. Ophunzira amayenera kukayamba kuchita umboni wawo muchikhalidwe chawo mu Yerusalemu ndi kuchulukana kukubzala mipingo madera ena omwe ali ndi chikhalidwe chawo. Kenako, ophunzira amayenera kuwoloka mayiko, malo mokumana anthu, ndi mipita momwe munali anthu kukafikitsa Uthenga Wabwino mudzikhaliidwe zotsiyanasiyana kuyambira ku samaliya ndikumathero konse kwa dziko lapansi (Macitidwe a Atumwi 1:8). Ophunzira anakwaniritsa kwachangu lamulo loti akachulukane kaye anthu achikhalidwe chawo (Macitidwe a Atumwi 2). Kukula kufikira zigawo zina zomwe zinali ndichikhalidwe chawo kunabwera potsatira mazunzo awo:

**... ndipo tsikulo kunayamba kuzunza kwakukuru pa mpingo unali m'Yerusalemu; ndipo anabalalitsidwa onse m'maiko a Yudeya ndi Samariya....**

**Pamenepo ndipo iwo akubalalitsidwa anapitapita nalalikira mauwo. (Macitidwe a Atumwi 8:1 ndi 4)**

Filipi anawolokoka mipata yazikhaliidwe napita pachitsitsimutso mu Samariya zomwe zalembedwa mu Macitidwe a Atumwi 8. Petro ndi Yohane anapitiridza utumiki mudera lomwe lija. Mtumwi Petro anali ndizovutazina pakuvomeredza ntchito yomwe anali nayo yakulalikira kuzikhaliidwe zina. Anali mu Yuda ozipereka ndipo poyamba analibe kuthekera kokhala ndi mayiko a anthu achikunja (Anthu omwe sanali Ayuda). Mulungu anaykhula ndi Petro kudzera maso phenya zomwe zalembedwa mu Macitidwe a Atumwi 10 ndipo kenako Petro anatengera Uthenga Wabwino kwa anthu achikunja omwe anali ku Kaisareya. Kukudza pakuwoloka mu Chipangano Chatsopano zafotokodzeredwa bwino ndi utumiki wa Mtumwi Paulo. Mulungu anamuyika mwapadera dera ku utumiki umenewu. Paulo anal mu Yuda, koma Mulungu anamuza kuti anali:

**... iye ndiye cotengera canga cosankhika, cakunyamula dzina langa pamaso pa amitundu ndi mafumu ndi ana a Israyeli. (Macitidwe a Atumwi 9:15)**

### **ZOLINGA ZA KUBZALA MPINGO**

Mwaphunira mbuyomu zolinga zaku lalikira. Zolinga za kubzala mpingo ndizofanana. Malingana ndi mene ikunenera Chipangano Chatsopano, cholinga pakuyamba kukudza mipingo zikuenera kuperekedwa kwa magulu a anthu omwe sanafikiridwepo, midzinda kenako midzi.

## MAYESO OZIYENSA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera.

---

---

---

2. Mau oti “Kukula mkati mwa mpingo” akutanthauzanji?

---

---

---

3. Mau oti “kukula kochulukitsa” kwa mpingo, kukutanthauzanji?

---

---

---

4. Mau oti “kukula kokudza” mu mpingo akutanthauzanji?

---

---

---

5. Mau oti “kukula kowoloka” mu mpingo akutanthauzanji?

---

---

---

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

## **ZOONJEZERA POPHUNZIRA**

1. Mukafuna kuphunzira zambiri za kukula mkati, kuchuluka, kukudza, ndi kukula kowoloka pezani phunziro la The Harvestime International Institute “*Njira zakuchulukitsa*”
2. Kuti mpingo uliwonse ukakule moyenera pakukudza, mpingo ukuyenera:

### **Kuvetsetsa cholinga chake ndi zoyenera kusatira:**

Pulogiramu kapena gulu lomwe layambitsidwa mpingo likuenera kukhala muumodzi ndi cholinga ndi zoyenera kusatira. Phunziro lamu The Harvestime International Institute “*kuchita ndi zolinga,*” limafotokodza bwino bwino.

### **Kuvetsetsa malamulo a baulo pa bungwe:**

Izi ndimonga mphatso za uzimu ndi gawo ndi kuphunzitsa otembenuka mwatsopano kuti akakhale atsogoleri awuzimu oyenera kuti angagwiritse ntchito mphatso zawo. Phunziro la The Harvestime International Institute “*kuchita pa malamulo a baibulo ndi kuchita ndi zolinga*” zikuthandizirani pakuchita izi.

### **Kuvetsetsa za zomwe baibulo likunena pazowayeneredza kukhala atsooleri:**

Phunziro la The Harvestime International Institute “*kuchita pa malamulo a baibulo,*” likufokodza moveka bwino.

### **Akaphunzitsidwe Madziko a Chikhulupiriro:**

Puphunziro la The Harvestime International Institute “*Kuimirira*” bukhu ili likakuthandizirani kuti mukafikire cholinga chanu.

### **Khanzikitsani mafunso olemba:**

Mukuenera kusatira izi:

- Khaziksana fundo ya chiphunzitso, kuti alendo akadziwe zikhulupiriro za baibulo za mpingo wanu.
- Pedzani zinthu zoyenera kumpingo kwanu zomwe boma limafuna.
- Mabungwe apa mpingo monga atsogoleri, achitetedzo, ndi dongosolo laza chuma.
- Dera ndi mwini wamalo ampingo.
- Ubale pakatia pa mpingo wawukulu ndimpingo omwe wakudzidwa.

## KUMAPETO

### MAWU OMALIZA...

...Kwa amene akuphunzira mu Harvestime International Institute.

Ngati mukuphunzira mu Harvestime International Institute ndipo mukutenga magawo onse omalidzika, ili ndi phunziro lomaliza mu bukhu la maphunziro akuphunzitsa. Pakudzera maphunziro amu the Harvestime mwapeza chinthu chachikulu pa chidziwitso ndi kuthekera komwe, mukagwiritsa bwino ntchito, muntha kukafikira dziko lanu lonse ndi Uthenga Wabwino.

Mukumbukire kuti, nthawi zina, kuti ndikovuta kusunga kuposa kupeza. “kupedza” ndiye kuti kutenga chithu chinachake. “kusunga” ndiye kuti kusunga ndi kugwiritsa ntchito. Kusunga nthawi zonse kumakhala kuti ndipakati pa chinthu chilichonse moyo. Sizili pa zomwe mwapedza koma pazomwe mukusunga ndicho chofunikira. Mwachitsanzo, sizikukwanira kungolandira Ambuye ngati pulumutsi wak, koma mukuenera kukhala mwa Iye kuti mukakhale ndikulimbikitsika kwa tsogolo lamayaya.

Baibulo limakamba zambiri za kusunga mu fanizo lomwe linanenedwa ndi Yesu mu Luka 19:12-26. Werengani ndime imene mu baibulo lanu. Mukaziwa kuti akapolo omwe anagwiritsa ntchito ndi kuchulikitsa ndalama anapatsidwa ndikulandira ndalama zambiri. Amene yemwe sanachite kathu ndi ndalama yomwe analandira ija anayiluzi. nkhanayi ikukamba kuti mukagwiritsa ntchito chomwe muli nacho chidzachulukidwa. Mukuenera kugwiritsa ntchito kapena kuyiluzi:

**Ndinena ndi inu, kuti kwa yense wakukhala naco kudzapatsidwa; koma kwa iye amene alibe kanthu, cingakhale cimene ali naco cidzacotsedwa. (Luka 19:26)**

Cholinga cha phunziro la Harvestime si kungopereka kuthekera kwa uzimu konga pa mwamba pa phiri kenako kukutumizani kuchigwa kuti mukachiluze. Kuthekera konga pamwamba pa phiri ndikukukozekeretsani inuyo pomwe muzakhale mu chigwa, ngakhaleso Mose anali nako kuthekera pa Phiri la Sinayi.

Kusunga zomwe mwaphunzira mu phunziro la the Harvestime, mukuenera kutenga zimenezi ndikupita nazo ku chigwa tsiku ndi tsiku la moyo wanu ndikutumikira ndikuzigwiritsira ntchito. Mukuenera kupitiridza phunziro lanu la Mawu a Mulungu ndi pephero. Mukuenera kugwiritsa ntchito ndondomekeo ya kututa muuzimu yomwe mwaphunzira ndi kufikira anthu ena kuwaphunzitsa zama dziko a chinkhulupiriro, mene angakhalire mu Ufumu wa Mulungu, mene anangaziwire liwu la Mulungu, ndi malamulo a nkondo za Uzimu.

Chifukwa ogwira ntchito yakututa muuzimu ndiwochepa, mukuenera kupitiridza kuphunzitsa ndikulalikira Uthenga Wabwino pamodzi ndikuwonetsera mphamvu ya Mzimu Woyera. Mukuenera kutsogolera ena kuti akadziwe mphatso zawo za Uzimu ndikugawana nawo malamulo amphamvu, atsimikizdzireni kuti akakhale ogwira ntchito amachawi. Mukuenera kuti musasiye kuchulukana, kukumana pamodzi, ndikusokhesa pamodzi zida za uzimu kuti mukagwiritse potuta minda ya dziko lapansi yomwe yaphsya.

Baibulo limatiphunzitsa kuti “kwa amene zochuluka zapasidwa, zambiritso zimayembekedzedwa.” Tapereka zambiri kupita ku manja pakudzera mumaphunziro a the Harvestime. Mukumbukira kuti ndime zonse zakhazikika pa malamulo oti “wina kuphunzitsa wina kufikira wina.” Mwafikiridwa pakudzera phunziro iyi. Tsopano ndi udindo wanu kuphunzitsa ena amene akatengeso udindo ophunzitsa ena:

**Ndipo zimene wazimva kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezi uikize kwa anthu okhulupirika, amene adzadziwa kuphunzitsa enanso. (2 Timoteo 2:2)**

Pamene mumayamba phunziro lanu la Harvestime, munatenga ganizo lofunikira kwambiri. Simunalowe muphunziro la chipembedzo kapena bungwe liri lonse. Munalowa muphunziro la “sukulu ya mzimu.” Ndiphunziro la mzimu wan ndi Mzimu Woyera—ndipo sukuluyi siyimantha.

Pamene mukumalidza phunziro lanu la Harvestime, simathero koma chiyambi. Sikuti ndi chikondwerero chopita class yina, koma kungoyamba chabe. Mwanola “chitsenga” chanu cha uzimu ndipo mwakudzeka kulowa munda kuti mukatute.

Monga momwe mwaphunzirira maphunziro anu, okolola amapita kumene zotuta zaphsya ndipo ndizokodzeka. Kumene mayatandidwe okatutawa atakutengereni, akudziwa ndi Mulungu yekha. Koma mukhale nako kulimbika koti simukugwira ntchito nokha. Mwalowa gulu la antchito achisirikali, kubwerera mbuyo kwa ophunzira a Yesu, amene anava mayitanidwe ndipo anayakha:

Ndinava kuyitanidwa, “bwera undisate”

.... anali omwewo.

Chimwemwe cha dziko chinakula;

Mzimu wanga unamusatira.

Ndinadzuka ndipo namusata....

.... anali omweo.

Dipo lamayitanidwewa, Mulungu yekha ndi amene adziwa, koma kumbukirani kuti mukuenera:

**Umve zowawa pamodzi nane monga msilikari wabwino wa Kristu Yesu. (2 Timoteo 2)**

Musakakhazikike pa chinthu chaching’ono koma pacholinga chomalidza. Pitirizani kubzala ndiku kolola, munthawi yofesa komanso munthawi yotuta, kufikira gulu liri lonse la anthu, ntundu uli wonse, ndi dziko liri lonse litafikiridwa ndi uthenga wabwino.

Musataye diso la maso phenya akututa muuzimu:

*“Ndipo linadza kwa ine maso phenya a munda ovungulira umene zokolola zake zinali zakuphsya zofikira kumalekedzero a dziko lapansi. Monga momwe ndimaona mutu uli onse wa tirigu unakhala mutu wa munthu; ndipo lamba lili lonse losatembenudzika, linakhala dzana lalitali.*

*Ambuye anandipasa...chitsenga chakuthwa cha Mau ake apa mtima. Anandiuza ine kuti ndiwokhese tirigu yense pamodzi, koma ndisagwiritse ntchito chitsenga podula kapena kupweteka okolola wina, ndisayakhe zonyoza zawo... koma ndigwire ntchito yomwe ndapasidwa ndikugwira ukadali usana.”*

-Aimee Semple McPherson, Mwini wake

-International Church of the Foursquare Gospel.

## MAYANKHO AMAFUNSO OZIYESA NOKHA

### CHAPUTALA 1:

1. Ndiposo anati, Ndidzafanizira Ufumu wa Mulungu ndi ciani? Ufanana ndi cotupitsa mikate cymene mkadzi anatenga, nacibitsa mu miyeso itatu ya ufa, kufikira unatupa wonsewo. (Luka 13:20-21)
2. Utumiki wonga chotupitsa ndi Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu kufalikira kuli konse kuli “linga” la dziko lapansi chifukwa mphamvu yotsatha ya Ufumu yonga mkate otupisa.
3. “Tanthaunzo la otayika” likunena kuti kuvetsetse kuti anthu onse amene sanalape machimo awo ndipo sanakumane ndikubadwa kwatsopano kwafotokodzedwa ndi Yesu mu Yohane 3 amanene kuti otayika chifukwa choti ataya chikhalidwe chopanda uchimo chomwe Mulungu anapereka pomulenga munthu. Tinthatso kunena kuti “ndiwo sapulumuka” kapena “osakhulupirira” chifukwa choti sanapulumutsidwe kuchokera kumachimo awo kudzera pakukhulupirira kuti Ambuye Yesu Kristu kuti ndi pulumutsi.
4. “Tsogola la anthu otayika” zikutanthauza kuvetsetsa kuti osapulumuka akakumana ndi imfa ya uzimu yomwe ili yolekanitsidwa ndi Mulungu kwamuyaya. Tsogolo lawo ndiku gahena.
5. -kupezeka                    -Kubzala  
-Kuvomeredza                -Kusandulizika  
-Kuumiridza                  -Kutenga mbali

### CHAPUTALA 2:

1. Mwina ndidzanena kwa oipa, iwe munthu oipa, ukuenera kufa ndithu, ndipo iwe sunamuchenjedze kamba ka khalidwe lake loipalo, munthu oipa azamfa mu uchimo wache, koma ndizakusungira mulandu iwe kuti wapha munthu. (Ezekiyeli 33:8)
2. -Lamulo                        -Kukhuzika  
-Gwirizano                    -Pikitsano  
-Kugwiritsa ntchito
3. Zinthu zitatu zofunika kuti mukakwaniritse ulamuliro wa kukalikira ndi:  
-Zikuenera ndikukhala ndicholinga choyamba.  
-Zikuenera kukapatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera.  
-Zikuenera kusatira dongosolo la Chipangano Chatsopano.



### CHAPUTALA 3:

1. Pakuti ndinapereka kwa inu poyamba, cimenenso ndinalandira, kuti Kristu anafera zoipa zathu, monga mwa malembo; ndi kuti anaikidwa; ndi kuti anaukitsidwa tsiku lacityatu monga mwa malembo. (1 Akorinto 15:3-4)
2. Mawu oti “Uthenga Wabwino” amatanthauza kuti “nkhani yabwino” tikamayankhula za Uthenga Wabwino kumabali ya baibulo, zimatanthaunza kuti khani yabwino ya Ufumu wa Mulungu ndi chipulumutso kudzera mwa Yesu Kristu.
3. Fundo zeni zeni za Uthenga Wabwino ndizoti Kristu anafera machimo athu malingana ndimalemba, Anayikidwa manda, ndi Anaukatso kwa akufa malingana ndi malemba. Ndi fundo yaying’ono kwambiri, Uthenga Wabwino utha kunenedwa muuthenga wa Yohane 3:16. Mumatathauzo akulu akulu, zimaphatikidzira zonse zimene Yesu anawaphunzitsa ophunzira ake.
4. i. Ntchimo ndila wina aliyese: Aroma 3:23  
ii. Chipulumutso chinabwera kwa aliyese: 1 Timoteo 2:4  
iii. Lamulo lakulapa ndila wina aliyense: Macitidwe a Atumwi 17:30  
iv. Kuyitanidwa kuti mukakhulupirire kwa wina aliyense: Aroma 10:9-11
5. Uthenga Wabwino ndiwaphamvu chifukwa:
  - Ndibvumbulutso la mphamvu ya Mulungu kwa munthu.
  - Umabweretsa chipulumutso kwa anthu onse, siwuona ntundu wa munthu, nkhungu la munthu.
  - Umabvumbulutsa chomwe chili choyenera kudziwa anthu chomwe chili cha Mulungu.
  - Umabvumbulutsa chiwerudzo ndi kwiyo wa Mulungu chifukwa cha ntchimo.
  - Umabvumbulutsa chilungamo cha Mulungu.
  - Umaoneretsa kuyeretsedwa (kukhululukidwa, kubwedzeresedwa mu ubale wabwino ndi Mulungu) kudzera kuchikhulupiriro.
  - Unakhazikika pa chikhulupiriro chomwe timakhalapo.

### CHAPUTALA 4:

1. **Pakuti Uthenga Wabwino sundicititsa manyazi; pakuti ulli mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa ali yense wakukhulupirira; kuyambira mYuda, ndiponso mheleni. (Aroma 1:16)**
2. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 4.
3. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 4.

4. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 4.
5. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 4.
6. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 4.
7. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 4.
8. Kuyikira umboni ndikunena zomwe waona ndi maso ako, zomwe wamva, kapena zomwe wakumana nazo. Ku bwalo lamalamulo, mboni ndi amene amanena za munthu kapena chinthu. Ngati mboni, tikunera kuyikira umboni za Yesu ndi dongosolo lake yopulumutsa ntundu onse wa anthu.
9. Mau oti “laity” akuthaunza kuti “kukhala mbali ya anthu otsakhidwa a Mulungu.” Tanthauzo leni la mau ndi “anthu onse a Mulungu.” Mau oti “munthu oyika” anabwera kugwiritsidwa ntchito kwa anthu amene samagwiria ntchito nthawi yoyikika padzochitika za mpingo.
10. Mau oti “akulu ampingo” anakhazikitsidwa pofuna kudzindikira akulu akulu otumikira pa mpingo. Kulu wa Mpingo amatanthauza kuti anthu amene amatenga utumiki ngati ntchito yawo ndi nthawi zina amalembedwa ntchito yokhazikika ndi mpingo.
11. Mayitanidwe a laity amatanthauza kuti ndi udindo wa okhulupirira aliyese kukakhala wansembe kapena wolalikira Uthenga Wabwino kwa anthu osakhulupirira.

#### **CHAPUTALA 5:**

1. Kuti ciyanjano ca cikhulupiriro cako cikhale camphamvu podziwa cabwino ciri mwa inu, ca kwa Kristu. (Filemoni 6)
2. Chiyanjano chakulalikira chikuenera:
  - Mungakhale njira zonse zaku thupi ndi zauzimu.
  - Zikhale za anthu onse mosatengera chuma.
  - Zifanane pakati pa gulu ndi munthu.
  - Zikhale zovetsetseka muchikhalidwe chawo
  - Ziposere kulakhula pakamwa pokha
  - Mukhale muumodzi ndi chikhalidwe cha moyo wanu
3. Macitidwe a Atumwi 26:18

#### **CHAPUTALA 6:**

1. Ndipo zimene wazimva kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezi uikize kwa anthu okhulupirika, amene adzadziwa kuphunzitsa enanso. (2 Timoteo 2:2)
2. Dongosolo la Mulungu lafotokodzedwa mu Macitidwe a Atumwi 1:8. Mzimu Woyera ndi mphamvu ya umulungu yomwe imathandizira njira yakuchulukitsa, Yesu Kristu akukhala pa phata pa uthenga ndipo dziko lonse likukhala mboni ya uthengawu. Okhulupirira akuyenera kukhala zotengera zakuchulukitsa. Dongosolo la Mulungu ndi loti okhulupirira aliyese akachitire “umboni” za Uthenga Wabwino, kuphunzitsa anthu omwe angakhale ndikuthekera koti nawoso akaphunzitse adzawo (2 Timoteo 2:2).
3. Andrew ndi Ananiya.

4. Zolinga za kulalikira ndi:
  - Zinthu zamakono
  - Kufikira manyumba
  - Anthu omwe sanafikiridwe
  - Madera otayika
  - Midzinda
  
5. Mitundu ya anthu ochima omwe anenedwa mu baibulo ndi:
  - Ochima mwadaladala
  - Ochima Osandulika
  
  - Ochimwa achipembedzo
  
  - Ochimwa okanidwa

#### **CHAPUTALA 7:**

1. ....omwe aja asanduliza dziko lokhalamo anthu, afika kunonso. (Macitidwe a Atumwi 17:6)
2. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 7.
3. Baibulo likunena kuti anachita “asanduliza dziko lokhalamo anthu” ndi Uthenga Wabwino.

#### **CHAPUTALA 8:**

1. Ndipo ndi mafanizo otere ambiri analankhula nao mau, monga anakhoza kumva. (Marko 4:3)
2. Fanizo ndi nkhani imene imagwira ngati chitsanzo kuchoka dziko akuthupi ndikukafotokodza za chowonadi cha uzimu. Tanthauzo leni leni la mau oti “fanizo” ndi “kukhala pambali” kapena “kufanizira.” Mu fanizo Yesu anagwiritsa ntchito chitsanzo chaku thupi ndiku fanizira chilungamo chaku uzimu. Faniziro ndi nkhani ya dziko lapansi lomwe limakhala ndi tanthauzo lakumwamba.
3. Kuvetsetsa chilungamo cha uzimu chomwe chimaphunzitsidwa mu fanizo kunaperekedwa kwa ophunzira chifukwa anali nawo malingaliro a uzimo. Amene analibe malingaliro awuzimu anava ma fanizo koma analephera kuwatathaunzira.
4. Onani kufotokodzedwa kwa fanizo mu chaputala 8.

#### **CHAPUTALA 9:**

1. ...asamariya ambiri anamkhulupirira Iye cifukwa ca mau a mkadzi, wocita umboniyo, kuti, anandiuza ine zinthu ziri zonse ndinazicita. (Yohane 4:39)
2. Ulaliki wa kwa munthu ndi mene dzina limanenera: ndikugawana Uthenga Wabwino munthu ndi munthu. Ndi munthu ndi munthu mzake, kulalikira kwa modzi modzi.
3. Ulaliki wakwa munthu umachita ndi:
  - Mboni yofasa
  - Galamukani
  - Mboni yam au

4. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 9.

#### **CHAPUTALA 10:**

1. Pakuti, cilengedwere dziko lapansi zaoneka bwino zosaoneka zace ndizo mphamvu yace yosatha ndi Umulungu wace; popeza zazindikirika ndi zinthu zolengedwa, kuti iwo adzakhale opanda mau akuwiringula. (Aroma 1:20)
2. Nthawi zina satana amayikidza mafunso ndi zowiringula mumaganizo a anthu. Nthawi zina anthu amapereka zowiringula zomwe sizili zawo. Anavapo munthu wina akupereka zowiringula zimene ndipo iwo akungofuna kuchedwesa kapena akufuna kuti kusitha nkhani. Anthu ena amapereka zowiringula zomwe zikuwakanikitsa kuti akapange chitsankho chosatira Kristu. Izi zikuenera kuti mukachite nazo pamene asanaande Uthenga Wabwino.
3. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 10.

#### **CHAPUTALA 11:**

1. Mu mphamvu ya zizindikilo ndi zozizwitsa, mu mphamvu ya Mzimu Woyera; kotero kuti ine kuyambira ku Yerusalemu ndi kuzungulirako kufikira ku Iluko, ndinakwanitsa Uthenga Wabwino wa Kristu. (Aroma 15:19)
2. Kulalikira kochulukitsa ndi kufikira kofalitsira Uthenga Wabwino omwe umagwira ntchito ngati chotupitsa mu mkate. Cholinga chake ndiku falitsa Uthenga Wabwino kufikira dera lonse litakwaniritsidwa ndi kukhuzika. Mukuenera kuyambira mumadera ang'ono ang'ono, kulalikira kochulukitsa kumafalikira kumidzi yamu dzinda wanu kapena nthawi zina ku dziko lanu.
3. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 11.
4. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 11.
5. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 11.
6. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 11.

#### **CHAPUTALA 12:**

1. Penyani mwa amitundu, penyetsetsani, nimudabwe kwakukuru, pakuti ndicita ntchito masiku anu, imene simudzavomera cinkana akufotokozerani. (Habakuku 1:5)
2. Chitsitsimutso chachikulu chimafikira anthu amene kwa zaka zambiri akhala akufunafuna Mulungu. Chimakhudza anthu amene sangathe kupita ku ntchalitchi. Chimapereka mwayi owonetsera mphamvu ya Mulungu kwa anthu osakhulupirira. Chimafikira anthu ambiri mwachangu ndi Uthenga Wabwino ndi njira yofunikira yofikira ntundu wa anthu ndi mene akuchuukira pa dziko lapansi. Kulalikira pa chitsitsimutso chachikulu zimakuthandizirani kuti mukaziwe malo omwe ali okodzeka ndizauzimu kuti mukakolole ndipo nthawi zina zimathera kubzalapo mipingo. Ngati pali kale mipingo pa derapo, kulula kumachitika pamene otembenuka mtima atsopano amawonjedzekera ku mpingo.
3. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 12.

#### **CHAPUTALA 13:**

1. Pomwepo Yesu anati kwa ophunzira ace, Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikane yekha, natenge mtanda wace, nanditsate Ine. (16:24)

2. Mau oti “otembenuka” amatanthauza kuti okhulupirira atsopano mwa Yesu amene abadwa mwatsopano mwachinkhulupiriro ndi kukhala mbali ya Ufumu wa Mulungu.
3. “Ophunzira” ndi otembenuka amene wakhazikitsidwa mu ziphunzitsa za chikhulupiriro cha ukristu ndipo ali ndi kuthera kokadzutsa otembenuka mtima atsopano ndikuwaphunzitsa. Mau oti “ophunzira” akutanthaunza kuti ophunzitsidwa, mwana wa sukulu, munthu amene amaphunzira pakutsatira munthu. Ndizoposa chiziwitso chakuva. ndikuphunzira kumene kumamukhunza ndikusitha moyo wa munthu.
4. Madera 6 akuyendera mwachangu:
  - Kutsimikidzika ku chipulumutso
  - kuvomeredza Yesu pagulu
  - Ubatizo wa madzi
  - Ubatizo wa Mzimu Woyera
  - Kukhala moyo odzipereka
  - Kukhala membala wa mpingo
5. Malamulo 9 ophunzitsiridwa amene ananedwa mu phunziro la Yesu ndi ophunzira ake ndi:
  - Kusankha
  - Kukhala ndi anthu
  - Kukonzekereso/Kupatura
  - Maso phenya
  - Malamulo
  - Kuwonetsera
  - Kutenga nawo gawo
  - Kutsogolera
  - kutumidza
6. Chowonadi chophunzitsa ndichimene chimachitika pamene simuli limodzi ndi ophunziara wanu. Kodi amapitiridzabe kukhala okhulupirika ndi kuphunzitsabe ena amene ali ndikuthekera kupitiridza dongosolo lakuchulukitsa?

#### **CHAPUTALA 14:**

1. Mzimu wa Ambuye uli pa Ine, Cifukwa cace Iye anandidzoza, Ine ndiuze anthu osauka Uthenga Wabwino; Anandituma Ine kulalikira am’singa mamasulidwe, Ndi akhungu kuti apenyenso, Kuturutsa ndi ufuru opwanyika. (Luka 4:18)
2. Kukodzekera kumakuthandizani kuti mukakhale kapolo wazeru wa Uthenga Wabwino ndi zinthu za utumiki monga, zomangamanga, katundu, ndi zida zamagesi, zachuma, ndi mphatso za uzimu za okhulupirira muchisamaliro chanu. Kukozekera kumapereka chitsogozo, zimakuthandizira kuti mukapange ziganizo zabwion, kukhazikitsa zolinga za utumiki, ndikukupangitsani kuti mukawunikire zinthu moyenera. Zimakuthandizirani kuti mukachite zinthu mwazeru kuposa posa kuchita makusokonekera.
3. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 14.

## **CHAPUTALA 15:**

1. ...akukhala naco cikondi comwe, a moyo umodzi, olingalira mtima umodzi; musacite kanthu monga mwa cotetana, kapena monga mwa ulemerero wopanda pace, komatu ndi kudzicepetsa mtima, yense ayese anzace omposa iye mwini; munthu yense asapenyere zace za iye yekha, koma yense apenyereenso za mzace. (Afilipi 2:2-4)
2. “Network” ndikubweretsa pamodzi ziduswa zambiri ndikupanga chinthu chomdzi. Kunena moveka bwino, network imapanga anthu kuyakhulana wina ndi mzake, kugawana zeru, nkhani ndi zipangizo kuti akakwaniritse cholinga chimodzi.
3. Werengani 12:4-13. Mu ndime imeneyi mpingo ukutengedwa ngati chiyanjano cha thupi ndikukhala nazo ziwalo zambiri ndi okhulupirira okhala ndi mphatso pogwira ntchito limodzi mu utumiki ndi ntchito. Ichi ndichisazo cha kugwirana zanja.
4. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 15.
5. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 12.
6. Chiyanjano cha mzimu.
7. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 15.

## **CHAPUTALA 16:**

1. Ndipo zizindikiro izi zidzakuwatsata iwo akukhulupirira; m’dzina langa adzaturutsa ziwanda; abzalankhula ndi malankhulidwe atsopano; adzatola njoka, ndipo ngakhale akamwa kanthu kakufa nako’sikadzawapweteka; adzaika manja ao pa odwala, ndipo adzacira. (Marko 16:17-18)
2. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 16.
3. Mitundu 5 yamatenda ndi:
  - Matenda a Uzimu
  - Matenda aku thupi
  - Matenda a malingaliro
  - Matenda odzunga bongo
  - Kudzuzidwa ndiziwanda
4. Machiritso a umulungu ndi pamene Mulungu modzi wachowonadi amazionetsera chikhulidwe chake, kukwaniritsa malonjedzano ake, ndi machitidwe ake pa chifundo chakuyelechedwa kwa Kristu pakuchiritsa munthu ndikumupangaso wangwiro mu Thupi, Lake, moyo, ndi mzimu.
5. Satana ndichiyambi cha matenda.
6. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 16.
7. Matenda ku ifa kapena matenda ku ulemerero wa Mulungu.
8. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 12.

## **CHAPUTALA 17:**

1. Anthu onse adziko lapansi akaziwa kuti ndinu ndani; mitundu yonse ikaziwa mene munapulumsira anthu anu. (Masalimo 67:2)
2. “Mbewu” ndi chinthu chomwe chimabweretsa zinthu zochuluka zosiyana siyana.
3. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 17.
4. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 17.

## **CHAPUTALA 18:**

1. Pamene mulikupita lalikani kuti, Ufumu wa Kumwamba wayandikira. Ciritsani akudwala, ukitsani akufa, konzani akhate, turutsani ziwanda; munalandira kwaulere, patsani kwaulere. (Mateyu 10:7-8)
2. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 18.
3. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 18.
4. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 18.
5. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 18.

## **CHAPUTALA 19:**

1. Ndipo pamene Iye anadziitanira ophunzira ace khumi ndi awiri, anapatsa iwo mphamvu pa mizimu yoipa, yakuiturutsa, ndi yakuciza nthenda iri yonse ndi zofoka zonse. (Mateyu 10:1)
2. Mizimu yopereka zilakolako, mizimu ya matenda, mizimu yoyipa.
3. Mphatso ya kudziwa mizimu imakuthandizani kuti mukaziwe mizimu yomwe ikugwira ntchito mwa anthu ena ndi mwachangu mukaziwe kuti munthu ali ndi mizimu oipa kapena ai omwe ukugwira ntchito mwa iye. Zimapewesa kuti mukakhuzidwa ndi zimu wazilakolako kapena mizimu yamaboza. Munthu amene ali ndi mphatso imenei antha kuziwa zichitochito ndi zolinga za mphamvu yaku midima.
4. Kukhala ndiziwanda ndi moyo oti munthu amakhala ndi chiwanda chimodzi kapena mizimu yoipa yambiri zimene zakhazikika mu munthu la munthu ndipo zimatenga ulamuliro onse wawukapolo.
5. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 19.
6. Kukhala ndichikhumbo khumbu cha ziwanda ndikukhala munthu oti zako zonse umafuna kuziwa ziwanda, satana ndi amithenga ake.
7. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 19.
8. Kuphinja ndi ziwanda ndikukhala pansa pa ulamuliro waziwanda, kubwera mosusa, kapena kumangidwa kuchokera kucha.
9. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 19.
10. Fanidzirani momwe mwafotokodzera pakunena fundo zanu mu chaputala 19.

## **CHAPUTALA 20:**

1. Kotere kuti munayamba kukhala inu citsanzo kwa onse akukhulupira m'Makedoniya ndi m'Akaya. Pakuti kuturuka kwa inu, kudamveka mau a Ambuye, osati m'Makedoniya ndi Akaya mokha, komatu m'malo monse cikhulupiriro canu ca kwa Mulungu cidaturuka; kotero kuti sikufunika kwa ife kulankhula kanthu. (1 Atesalonika 2:7-8)
2. Mawu oti “mpingo” akutanthaudza “kukumana kwa anthu amene ali a Ambuye” kapena “anthu amene ayitanidwa.” Mawu oti “mpingo” agwiritsidwa kukumano wa anthu amene ali gawo lalikulu, nthupi lonse la Kristu.
3. Yesu Kritsu ndi mutu wa mpingo.
4. Ndi onse amene ali obadwa mwatsopano, ndi anthu amene ayitanidwa “Mwala wamoyo” mu 1 Petro 1:5
5. Atumwu, aneneri, alaliki, abusa, ndi aphunzitsi (Aefeso 4:11-16)
6. Cholinga cha mpingo ndi:

- Kulalikirira: Ophunzira anali okangalika ndikulaikira ndikuphunzitsa Uthenga Wabwino, kubatidza otembenuka mtima kumene, kuwatsogoleri ku ubatidzo wa Mzimu Oyera, kuchiritsa odwala, kumasula ndikuchotsa ziwanda.
- Kukozekeretsa: Kuyeretsa ndikutanthauza kuti kuwumba. Okhulupirira anabzala mipingo kuti akaphunzitse komanso kuyendetsa otembenuka atsopano kufikira ata kwima muuzimu ngati ophunzir

7. Mpingo waku Atesalonika.

### **CHAPUTALA 21:**

1. Kwa Iye ukhale ulemerero mu Mpingo ndi mwa Kristu Yesu, kufikira mibadwo yonse ya nthawi za nthawi. (Aefeso 3:21)
2. Njira 10 zakubzala mipingo modzungulira ndi:
  - Ogwira Ntchito Kutumizidwa
  - Anthu Kufikiridwa
  - Uthenga Wabwino Kuperekedwa
  - Kutembenuka Mtima Kwa Akuvera
  - Kutsokhana Kwa Okhulupirira
  - Kusimikidzika Kwa Chinkhulupiriro
  - Kusankha Atsogoleri
  - Mpingo Kutsimikdzika
  - Ubale Kupitirira
  - Kupitiridza Uthenga
3. Zolinga 7 za utumiki wa Mtumwi Paulo zinali:
  - Midzinda
  - Minda Yotayika
  - Anthu ake omwe
  - Anthu osafikiridwa
  - Magulu a Anthu
  - Mitsokhano ikulu ikulu ya Uthenga Wabwino
  - Kuphunzitsa modzi modzi

### **CHAPUTALA 22:**

1. Kucokera kwa Iye amene thupi lonse, lothandidzidwa pamodzi mwa mfundo ndi mitsepha, likula ndi makulidwe a Mulungu. (Akolose 2:19)
2. Kukula mkati mwa mpingo, tikutathauza kukula mzimu ndi kukula kwa mamembala ake. Mpingo umakula mzimu molingana ndikukula kwama membala ake.
3. Kukula kochulukitsa kumachitika pamene okhulupirira atembenuka mtima munthu kupita kwa Kristu ndikuwabweretsa kuchiyanjano ndi anthu mupingo mwawo momo. Ichi chimabweretsa kukula mu nambala yampingo muderalo



4. Kukula kokudza kumachitika pamene mpingo wayambitsa mpingo wina muchikhalidwe cha anthu omwewo. Mpingo watsopano umakhala okudza “mayi” mpingo, ngati mwana wakuthupi ndikukula kwa makolo ake
5. Kukudza kowoloka kumachitika pamene mpingo wawonjedzekereka kufika kudziko, malo okumaniramu anthu, tundu wa anthu, kuti mukadzale mpingo watsopano muchikhalidwe chotsiyana